

NDONDOMEKO

ZA

MPHAMVU

HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a Harvest International Institute ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

@Harvestime International Institute

ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe Ntchito Ka Bukuli.....	3
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu.....	4
Mau Otsogolera.....	5
Zolinga za Maphunzirowa.....	7
1. Moyo winawo ukatha moyo uno.....	8
2. Kochokera Mphamvu.....	22
3. Kulimbana ndi Chinyengo.....	35
4. “Palibe Munthu Anayankhula ngati Iye”.....	51
5. Mphamvu Yopatsidwa.....	60
6. Cholinga cha Mphamvu.....	69
7. Ndondomeko ya Mphamvu 1: Mphamvu ya Uthenga Wabwino.....	86
8. Ndondomeko ya Mphamvu 2: Mphamvu ya Mzimu Woyera.....	95
9. Ndondomeko ya Mphamvu 3: Mphamvu ya Chikondi.....	106
10. Ndondomeko ya Mphamvu 4 : Mphamvu ya Kudzodzodzedwa ndi Mphamvu.....	116
11. Ndondomeko ya Mphamvu 5: Mphamvu, Chikhulupiriro, ndi Ntchito.....	131
12. Ndondomeko ya Mphamvu 6: Mphamvu mu Dzina la Yesu.....	139
13. Ndondomeko ya Mphamvu 7: Mphamvu ya Pemphero.....	157
14. Ndondomeko ya Mphamvu 8: Mphamvu ya Mau.....	188
15. Ndondomeko ya Mphamvu 9: Mphamvu ya Ulamuliro.....	199
16. Ndondomeko ya Mphamvu 10: Mphamvu ya Kuuka Kwa.....	212
17. Ndondomeko ya Mphamvu 11: Mphamvu ya Mazuzo.....	220
18. Mmene Mungakumanirane ndi Mphamvu ya Mulungu.....	236
19. Kulephera kwa Mphamvu.....	243
20. Kukumana ndi Zotchinga.....	253
Mayanko Amayeso Odziyesa nokha.....	262

KAGWIRITSIDWE NTCHITO KA BUKULI

KAKONZEDWE KA BUKULI

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

Zolinga: Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Werengani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

Vesi Yotsogolera: Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

Zopezeka mu Magawo: Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

Mayeso Odziyesa Nokha: Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

Zophunzira Zowonjezera: Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mawu Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

Mayeso Omaliza: ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

ZOWERENGA ZINA ZOFUNIKA POPHUNZIRA PHUNZIROLI

Mudzafunikira Buku Lopatulika

NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

MKUMANO WOYAMBA

Kutsekulira: Yambani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu: Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene muzikumana.

Mayamiko ndi Matamando: Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

Gawani Mabuku Kwa Ophunzira: Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

Perekani Ntchito Yoyamba. Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene aziphunzitsidwa pa mkumano uli wonse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

Kutsekulira: Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina a ophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a ophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

Kukumbutsira: Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

Phunziro: Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso m'mene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi utumiki.

Mayeso Odziyesa Nokha: Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankho kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipezere okha mayankho.

Mayeso omaliza: Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina aliyense ali ndi buku laphunziroli.

PHUNZIRO: NDONDOMEKO ZA MPHAMVU

MAU OTSOGOLERA

Yesu anawauza atsogoleri ampingo wa Chipangano Chatsopano...

Koma Yesu anayankha, nati kwa iwo, Mungolakwa a osadziwa malembo, kapena mphamvu za Mulungu. (Mateyu 22:29)

Chowonadi chauthenga wabwino chiri pawiri. Choyamba, ndi mau a Mulungu omwe anawonetseredwa mu Baibulo. Kuti mudziwe malemba mukuyenera kuphunzira, kumvetsetsa, ndikuwagwiritsa ntchito.

Koma choonadi chauthenga wabwino ndi chakuti chimaposa malemba. Ndipo ndi mphamvu ya Mulungu. Kuti mudziwe mphamvu ya Mulungu mukuyenera kumvetsetsa ndi kugwiritsa ntchito ndondomeko za mphamvu. Mphamvu ya Mulungu ikuyenera kuti ikhale yeni yeni m'moyo mwanu pakudzera mu zomwe mwakumana nazo.

Mpingo woyamba unabadwa powonetsera mphamvu ya Mulungu, osati kudzera pakuyankhula bwino kapena mtsutso wakuphunzira mau a Mulungu. Paulo analemba:

Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'cionetso ca Mzimu ndi ca mphamvu; kuti cikhulupiriro canu cisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu. (1 Akorinto 2:4-5)

Paulo anazindikira kuti...

Pakuti ufumu wa Mulungu suli m'mau, koma mumphamvu, Mufuna ciani? (1 Akorinto 4:20)

Yesu anawasiyira okhulupirira ntchito yaikulu yoti akafikire dziko lonse ndi uthenga wabwino wa ufumu. Ntchito iyi singatheke ndi mau chabe okha. Monga ngati mmene zinaliri ndi mpingo woyamba, lereso pakuyenera kuti mphamvu ya Mulungu iwonetseredwe.

Anthu ambiri amadziwa mau a Mulungu koma sanakumane ndi mphamvu ya Mulungu. Samamvetsetsa mphamvu ya uthenga wabwino. Atumiki ambiri ndi ophunzira bwino. Amalarikira ndi mau okopa kwambiri chifukwa cha nzeru za umunthu zomwe alinazo, koma popanda kuwonetsera mphamvu ya Mzimu Woyera.

Mipingo ina zozizwa zinasithanitsidwa ndi maganizidwe aumunthu amene amafuna kuti china chilichonse chifotokozedwe bwino mmene chachitikira. Mphamvu zasithanitsidwa ndi mkambirano omwe umakhalapo okhudza zophunzira za umulungu pomwe pamakhala mtsutso okuti ngati zozizwa leronso zimachitikabe kapena zinali za mpigo woyamba basi. Pamene kuganizo ndi mtsutso zikutenga malo azozizwa, moyo oyenda ndi Mulungu unasithanitsidwa ndi chipembedzo chapanga munthu. Anthu ali ndi mavetsedwe a chipembedzo chawo ndipo zimatsatiridwa ndi miyambo. Amafuna kuti akumanea ndizoona zenizeni.

Ngati chikhulupiriro chanu chimaina pa mphamvu ya Mulungu mmalo mwa nzeru ya munthu, mukuyenera kukumana ndi kuyenda kwamphamvu monga momwe zimkachitikira ndi mpingo woyamba. Okhulupirira mu mpingo woyamba....

Ndipo iwowa anaturuka, nalalikira ponse ponse, ndipo Ambuye anacita nao pamodzi, natsimikiza mau ndi zizindikilo zakutsatapo, Amen. (Marko 16:20)

Tanena zomugwirira ntchito Mulungu. Timakonzekera utumiki wanthu ndipo timamupepha Mulungu kuti audalitse. Koma malingani ndi Baibulo pofuna kukhala ndi utumiki opambana ndizakuti Mulungu akuyenera kugwira nafe ntchito, potsimikiza mau ake ndi zizindikiro za zozizwa.

Dziko silikopeka ndi zomwe mukuchita kwa Mulungu. Dziko limakopeka ndi Yesu pamene akuwona zotsatira zowoneka za mphamvu ya Mulungu yomwe yasitha moyo wanu. Dziko limakopeka ndi kuwonetsera kwa mphamvu ya uzimu pamene Mulungu akugwira nanu ntchito amafuna kuti atsimikiize mau Ake ndi zozizwa.

Ndondomeko ya mphamvu yomwe yaphunzitsidwa mu phunziro iri ikuthandizirani inu kuti mukumane ndi mphamvu za uzimu zomwe zakambidwa mu Baibulo. Phunziro iri likuyakha kulira kwa mtima kwa onse amene akumva njala kuti amve zoonna mmalo mwa chipembedzo. Ikusuthani inu kuchoka kungokhala wowonerera ndikukhala amene muziwonetsera mphamvu ya Mulungu.

ZOLINGA ZA MAPHUNZIROWA

Pomaliza pa maphunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kuwonetsa komwe mpamvu za uzimu zimachokera.
- Kuzindikira mpamvu zachinyengo za mdani.
- Kufotokoza mwachidule mpamvu zomwe Mulungu anapereka kwa Yesu.
- Kulandira ulamuliro omwe Yesu anapereka kwa okhulupirira.
- Kufotokoza cholinga cha Baibulo pa za Mpamvu za uzimu.
- Kofotokoza ndi kugwiritsa ndondomeko za mphamvu zotsatirazi:
 - Mphamvu ya uthenga wabwino
 - Mphamvu ya Mzimu Woyera
 - Mphamvu yachikondi
 - Kudzodza kwa mphamvu
 - Mphamvu, chikhulupiriro, ntchito
 - Dzina la Yesu
 - Mphamvu ya pemphero
 - Mphamvu ya Mau
 - Kukhala olamulira pamene ukulamuliridwa
 - Mphamvu ya kuuka Kwake
 - Chiyanjano muzowawa zake
- Kufotokoza mphamvu ya Mulungu mmoyo mwanu ndi mu utumiki
- Kuwonetsera zifukwa zakulephera kwamphamvu.
- Kukumana ndi zotchinga ndikugonjetsa satana pamene akutsutsana ndi ulamuliro wanu wa Uzimu.

CHAPUTALA 1

MOYO WINAWO UKATHA MOYO UNO

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera kuchokera pamtima.
- Kofotokoza kusiyana kwachipembedzo ndi kuwonetseredwa kweni kweni kwa mphamvu za Mulungu.
- Kuloza mmene mphamvu za kudziko ziriri.
- Kupereka kusiyana komwe Baibulo limafotokoza pakati pa mpamvu zakudziko ndi za Baibulo.
- Kufotokoza mphamvu za m’Baibulo.
- Kulozera mphamvu zaposa chilengwe zomwe ndi gwero la mphamvu za uzimu.
- Kulozera magawo awiri a malonjezano a Baibulo.
- Kulemba pansi ndondomeko zotengera malonjezano a Mulungu.

VESI YOTSOGOLERA

Inu Mulungu, ndinu Mulungu wanga; ndizakufunani m’matanda kucha: Moyo wanga ukumva ludzu la kwa Inu, thupi langa lilirira Inu, Mdziko louma ndi lotopetsa, lopanda madzi. Kuti ndione mphamvu yanu ndi ulemerero wanu, monga ndinakuonani m’malo oyera. (Masalimo 63:1-2)

MAU OYAMBA

Monga mmene liriri tulo ndi kutethera kwachinyengo komwe kumabwera kwa munthu yemwe akufa chifukwa chakuzizira ,zirinso chimodzimodzi ndi dziko la uzimu. Kulizotchinga ndimachitachita osakhudzika pamene anthu akumwalira mu uzimu.

Chipembedzo ndikuyesayesa kwa munthu kuti adziwe Mulungu. Ndizochitachita ndi malamulo, ntchito ndi mau koma zopanda mpamvu. Chipembedzo chimabweretsa imfa yaku uzimu.

Mphamvu ya Mulungu imawonetseredwa pakufuna kuti Mulungu aziwonetsere Yekha kwa munthu. Mphamvu za Uzimu ndi ufumu wa Mulungu imabweretsa moyo wa Uzimu.

Ambiri akumana ndichipembedzo. Olowa magulo ndi zipembedzo zosiyanasiyana. Mabungwe amenewa awalowetsa anthu mu zinthu zomwe sizikhudzanso ndi zauzimu. Anthu otere amakhala asanakumane ndi mphamvu ya uthenga wabwino yomwe ingathe kusitha miyoyo yawo. Iwowo ndiongonjetsedwa ndiponso ofoketsedwa, ndiodwalika ndiponso amvulazidwa. Akufa kuuzimu. Mitima yawo iri monga momwe Davide analemba Salimo....

Inu Mulungu, ndinu Mulungu wanga; ndidzakufunani m'matanda kuca: Moyo wanga ukumva ludzu la kwa Inu, thupi langa lilirira Inu, M'dziko louma ndi lotopetsa, lopanda madzi. Kuti ndione mphamvu yanu ndi ulemerero wanu, Monga ndinakuonani m'malo oyera. (Masalimo 63:1-2)

Anthu awa akuyenera kuti akumane ndi moyo potsatira chipembedzo.

MITUNDU YA MPHAMVU

Pali mitundu yambiri ya mphamvu mu dziko lero:

Mphamvu za ndale zimakhala ndi amene akulamulira bungwe, mtundu, mudzi, matauni, dera, gawo la ndi dziko lonse.

Mphamvu za maphunziro aukachenjede zotsatira pakupeza zinthu zatsopano, zolemba ndi kupanga zamaimbidwe, komaso kukhazikitsa masukulu aukachenjede.

Mphamvu za kuthupi zimenezi zimakhala ndi anthu Amene ali ndi mphamvu, ambirimwa iwo amakhala akatswiri amipikisano yosiyanasiyana.

Mphamvu ya pazachuma mphamvu zimenezi zimakhala ndi ama banki, azamalonda amene ndi olemera kwambiri.

Mphamvu yapa zakhondo zimakhala ndi asilikira opambana zomwe amagwiritsa ntchito poziteteza komaso pakupeza madera ena atsopano.

Mphamvu za mphamvu zimathandiza anthu munjira zambiri kuyambira ku moto wawamba omwe anthu amawotha kukafikira magetsi omwe amagwiritsidwa ntchito mu nzinda onse.

Mphamvu zachipembedzo yomwe imapangitsa kuti pakhale ma kachisi ndi chikhalidwe chopembedza.

Zonsezi ndi mphamvu zapamwamba kwambiri zomwe zikugwira ntchito lero mudziko mwanthu. Koma kuitana kwa Yesu sikumphamvu zaku dziko. Ndi mphamvu za Uzimu. Ndi mphamvu zomwe sizimafusa “kodi ndingakhale bwanji wamkulu?”, mmalo mwake “kodi ndingatumikire bwanji?”

KUSIYANA KWA MPHAMVU MMENE ZIRIRI

Yesu anafotokoza kusiyana kwa mmene mphamvu zakudziko ndi za ufumu wa Mulungu. Iye anati:

Koma Yesu anawaitana, nati, Mudziwa kuti mafumu a anthu amadziyesa okha ambuye ao, ndipo akuru ao amacita ufumu pa iwo. Sikudzakhala comweco kwa inu ai; koma amene ali yense akafuna kukhala warnkuru mwa inu, adzakhala mtumiki wanu; ndipo amene ali yense akafuna kukhala woyamba mwa inu, adzakhala kapolo wanu: monga Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa koma kutumikira, ndi kupereka moyo wace dipo la anthu ambiri. (Mateyu 20:25-28)

Kuyitana kwa Yesu ndiye kuchoka ku mphamvu ya dziko ndikupita ku mphamvu ya Uzimu yomwe imaperekedwa ndicholinga chotumikira ozuzika, otaika, ndi dziko lakufa.

MPHAMVU YA UZIMU

Pamene tikuyakhula za mphamvu mu phunziro ili, tikunena za momwe Baibulo limawonera za mpamvu za uzimu. Tanthauzo la Baibulo pa mau oti “mphamvu” ndi zazikulu za uzimu, kuthekera, ndi mphamvu. Ndizoposa chilengedwe zomwe zimabweretsa zotsatira zazikulu ndi zozizwa.

Mau enanso ndi “ulamuliro”, agwiritsidwanso ntchito muphunziro ili. Monga mu Baibulo, zirinso chimodzimodzi ndipo liri ndi tathauzo lofanana ndi “mphamvu.” Ulamuliro ukutathauza kuti zovomerezeka ndi mphamvu zolondola zoti ukhoza kugwira ntchito mmalo mwa wina. Kutenga ulamuliro ndi njira yowonetsera mphamvu komanso ndikukhala ndi ufulu ogwiritsa ntchito mphamvu zopatsidwa mkatimkati mwa malire opatsidwa.

MACHITACHITA AMPHAMVU ZA UZIMU

Pali mpamvu zambiri zomwe zimagwira ntchito ku uzimu. Gwero la Baibulo la mphamvu za Uzimu ndi Mulungu amene ndi owona komaso wamoyo amene wawonetseredwa mu Baibulo.

Mwa Mulungu muli atatu amene ndi Mulungu Atate, Mulungu Mwana Yesu Kristu, ndiposo Mulungu Mzimu Woyera. Mulungu Atate nde chiyambi champhamvu.

Anthu onse amvere maulamuliro a akulu; pakuti palibe ulamuliro wina koma wocokera kwa Mulungu; ndipo iwo amene alipo aikidwa ndi Mulungu.

(Aroma 13:1)

Mulungu wapereka mphamvu kwa Mwana wake, Yesu Kristu:

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko. (Machitidwe 1:8)

Mphamvu ina ndi mphamvu ya uzimu, koma ndi mpamvu yoyipa. Ndi gwero la choipa cha mphamvu ya uzimu ndipo ndi gwero la ufiti, zanyanga ndi zonse zoipa.

Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefenso 6:12)

Muphunzira zambiri pa “zampamvu zachinyengozi” pofuna kufanana ndi mphamvu za Mulungu mu chaputala 3 cha maphunzirowa.

KUWONETSERA KWA MPHAMVU

Pamene Yesu anayamba utumiki wake wa paliponse, unali utumiki wa zozizwa. Utumiki wake sunapambane chifukwa choti anali ndi dongosolo la bwino. Anayamba ndi ophunzira khumi ndi awiri koma anamaliza ndi khumi ndi modzi. Sunapambane chifukwa chakutchuka. Pamapeto pake, aliyense anamukira kuphatikizapo omutsatira Ake. Utumike wake unakhudza anthu ambiri chifukwa chakuti mphamvu zinawonetseredwa.

cifukwa mau ace anali ndi ulamuliro. (Luka 4:32)

Ndipo anthu onse anadabwa, nalankhulana wina ndi mnzace, nanena, Mau amenewa ali otani? cifukwa ndi ulamuliro ndi mphamvu angolamulira mizimu yonyansa, ndipo ingoturuka. (Luka 4:36)

za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Machitidwe 10:38)

Mpingo woyamba unabadwa chifukwa chowonetsera mphamvu. Zinanenedwa za iwo:

Pamene sanawapeza anakokera Yasoni ndi abale ena pamaso pa akuru a mudzi, napfuula kuti, Omwe aja asanduliza dziko lokhalamo anthu, afika kunonso; (Machitidwe 17:6)

Mpingo woyamba unakhudza mizinda ndi maiko onse, koma sanachite izi pongolalikira pokha. Anthu anamvetsera mwachidwi ndipo miyoyo inasithika chifukwa anawona machitamachi amphamvu ya Mulungu.

Ndipo makamuwo ndi mtima umodzi anasamalira zonedwa ndi Filipo, pamene anamva, napenya zizindikilo zimene anazicita. Pakuti ambiri a iwo akukhala nayo mizimu yonyansa inawaturukira, yopfuula ndi mau akuru; ndipo ambiri amanjenje, ndi opunduka, anaciritsidwa. Ndipo panakhala cimwemwe cacikuru m'mudzimo. (Machitidwe 8:6-8)

Pamene Petro anapita ku Lydda, anapezako munthu wina dzina lake Aenas amene anakhala akudwala kwa zaka zisanu ndi zitatu.

Ndipo Petro anati kwa iye, Eneya, Yesu Kristu akuciritsa iwe; uka, yalula mphasa yako. Ndipo anauka pomwepo. Ndipo anamuona iye onse akukhala ku Luda ndi ku Sarona, natembenukira kwa Ambuye amenewa. (Machitidwe 9:34-35)

Ku Yopa, Petro anadzutsa mzimai wina dzina lake Dorika kuchokera kwa akufa. Pamene chozizwa chinachitika...

Ndipo kudadziwika ku Yopa konse: ndipo ambiri anakhulupirira Ambuye. (Machitidwe 9:42)

Chozizwa chinachirichonse chimaonetsera mphamvu ya Mulungu yomwe inakhazikika kwambiri pa Yesu Kristu. Mphamvu ina iriyonse imakunama ndizotsatira pakuchuluka kwa mpingo.

Machitachita azandale siamene akufunika kuti uthenga ukathe kufikira dziko lonse. Mpingo woyamba unalibe kuthekera koti unakamutulutsa Petro kundende, koma unali ndi mphamvu zambiri pakumpempherera iye kuti atuluke.

Kulalikira kwambiri sikuti ndikomwe kukakhudze maiko. Mpingo woyamba unapemphera kwa masiku ambiri, kenako anakalalikira kwa mphindi zochepa zokha, ndipo anthu 3000 anapuluma (Machitidwe 1:2). Koma masiku ano timangopephera kwa mphindi khumi zokha koma mkukulalikira kwa masiku khumi mapeto ake anthu makumi atatu okha ndamene amatembenuka mtima.

Utumiki kukhala ndi ndalama zochuluka sichitsimikizo chakuti uthenga wabwino ofikira dziko lonse. Ngakhala chili chilungamo kuti ndalama zimafunika pa ntchito za utumiki, koma sikuti ndizofunika kwambiri kuposa china chilichonse.

Pamena Petro ndi Yohane amkadutsa pa khomo lakachisi ku Yerusalemu, opepha wina wolumala anawapepha ndalama zochepa. Petro ndi Yohane analibe ndalamazi, koma anapereka chomwe anali nacho.

Koma Petro anati, Siliva ndi golidi ndiribe; koma cimene ndiri naco, ici ndikupatsa, M'dzina la Yesu Kristu Mnazarayo, yenda, Ndipo anamgwira Iye ku dzanja lace lamanja, namnyamutsa; ndipo pomwepo mapazi ace ndi mfundo za kumapazi zinalimbikitsidwa. Ndipo anazunzuka, naimirira, nayenda; ndipo analowa pamodzi nao m'Kacisi, nayenda, nalumpha, nayamika Mulungu. (Machitidwe 3:6-8)

Chomwe anali nacho ndi mphamvu ndi ulamuliro mu dzina la Yesu. Analibe ndalama zoti akalengezere kuti akafikire mzinda onse wa Yerusalemu. Analibeso ngakhale timabuku ndi Baibulo, analibeso olo kanema. Koma anali ndi mphamvu. Pakudzera kuwonetsedwera kwa mphamvu ya Mulungu, mzinda onse unakhudzidwa ndi Uthenga wabwino (Machitidwe 3-4)

Mpingo woyamba unazindikira kuti uthenga wa ufumu sunali wa mau okha komaso ndi mphamvu zomwe.

Mwadzala kale, mwalemerera kale, mwacita ufumu opanda ife; ndipo mwenzi mucitadi ufumu, kuti ifenso tikacite ufumu pamodzi ndi inu. Pakuti ufumu wa Mulungu suli m'mau, koma mumphamvu, Mufuna ciani? (1 Akorinto 4:20)

MPHAMVU YAKUSAKHA

Pamene Mulungu analenga dziko, anapanga zinyama zambiri zosiyanasiyana. Anapanga nyama, nsomba, zouluka, ndi mbalame (Genesis 1). Koma cholenga chopambana chomwe Mulungu analenga mu chifaniziro chake ndi munthu. Munthu ndi oposa cholengedwa chilichonse chifukwa ali ndi nthupi, moyo, ndi mzimu. Analengedwa kuti akamulambire Mulungu ndikutinso akakhaleso naye paubale (Genesis 2-3).

Munthu, pachilengedwe, ndi bwenzi la Atate Mulungu wa zozizwa, Mulungu wowona ndi wamoyo. Munthu, anauzilidwa mphweya wa Mulungu ndipo anapangidwa mchifaniziro Chake, ali ndi mphamvu kuposa zolengedwa zina. Kuchita zozizwa chikuyenera kukhala chikhaliidwe chake.

Munthu ali ndi maganizo anzeru za uMulungu. Munthu ali ndi mphamvu yosakha. Munthu akhoza kusakha kuchita kapena kusachita choipa. Akhoza kusakha kumvera Mulungu kapena Satana. Yesero loyamba la munthu linachitika m'munda wa Ideni linakhazikika kwambiri pa mphamvu yakusakha (Genesis 3). Chifukwa chachisankho cholakwikwa, tchimo lomwe Adamu anachita limayendabe mpakana lero kwa anthu onse.

MAZIKO AMPHAVU YA UZIMU

Ngati munthu akufuna kukumana ndi mphamvu yeni yeni ya uzimu, akuyenera kusakha kumvera Mulungu. Pakuti onse ndiochimwa, nde onse akufunika chikhululukiro.

Kusakaza ndi kusauka kuli m'njira zao; pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu; (Aroma 3:23)

Chikhululukiro chimabwera pakulapa ndikukhulupirira mwa Yesu Kristu.

Tikati kuti tiribe ucimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi. Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. (1Yohane 1:8-9)

Kulapa machimo ndimaziko a mphamvu za Uzimu. Simungakumane ndi mphamvu ya Mulungu ngati mukupitiriza kukhalabe mu imfa ya uzimu mmachimo.

Pamene ophunzira anali mu mzinda wina, munthu wina otchedwa Simon anawona mphamva ya Mulungu ikugwira ntchito. Anampatsa Petro ndalama ndipo anati:

Koma panali munthu dzina lace Simoni amene adacita matsenga m'mudzimo kale, nadabwitsa anthu a Samariya, ndi kunena kuti iye yekha ndiye munthu wamkuru; (Machitidwe 8:19)

Petro anayakha:

Koma Petro anati kwa iye, Ndalama yako itayike nawe, cifukwa unalingirira kulandira mphatso ya Mulungu ndi ndalama. Ulibe gawo kapena colandira ndi mau awa; pakuti mtima wako suli wolunjika pamaso pa Mulungu. Cifukwa: cace lapa coipa calm ici, pemphera Ambuye, kuti kapena akukhulukire iwe colingiriraca mtima wako. Pakuti ndiona kuti wagwidwa ndi ndulu yowawa ndi nsinga ya cosalungama. (Machitidwe 8:20-23)

Kulapa ndi maziko amphamvu zenizeni za uzimu. Simungawone mphamvu ya Mulungu ngati koyamba simunalape. Chipulumutso kumachimo ndi chinthu chachikulu chomwe chimawonetsera mphamvu ya Mulungu.

Mulungu samapereka mphamvu yake kwa munthu ochimwa. Samagwiritsa ntchito anthu amene amayesa kusitha miyoyo yawo paokha (Mateyu 9:16-17). Mulungu amawonetsera mphamvu yake kudzera mwa zotengera zomwe ziri zoyera, amene alapa ndipo akumtumikira Iye.

KUTENGA MALONJEZANO

Okhulupirira alonjezedwa mphamvu za Uzimu, koma pali mbali ziwiri za malonjezano aliwonse a Mulungu:

Lonjezano: zopezeka, mau eni eniwo, ndi tanthauzo la lonjezano.

Kutenga lonjezanolo: sungagwiritse ntchito chomwe ulibe. Ndikofunika kuti mufuse lonjezano kwa Mulungu ndicholinga chakuti likhale lowoneka ndimaso mmoyo wanu.

Kodi mungafunse bwanji malonjezano kuchokera kwa Mulungu? Ndendomeko zake ndi izi:

1. MUKUYENERA KUSAKHA KUTERO:

Muli ndi mphamvu yomvomera malonjezano a Mulungu, kuwakana ndi kuwanyalanyaza. Anthu ambiri akana lonjezano la mphamvu ya Uzimu. Amakhulupirira kuti inali ya mpingo woyamba wokha basi. Pamene ena sanailabadireso. Amawerenga malonjezano mu Baibulo, koma

samachitapo kanthu pa iwo. Anthu oterewa sanawonepo mphamvu ya Mulungu miyoyo yawo chifukwa alephera kufusa malonjezano kwa Mulungu.

Ngati pali lonjezano la mau a Mulungu lomwe silinakwaniritsidwe moyowanu, sizikutathauza kuti lonjezanolo silowona kapena silanu. Musamatanthauzire Baibulo malingana ndi zomwe inuyo mukukumana nazo. Chifukwa chakuti lonjezano la Mulungu silinabwere pa moyo wanu izi sizikutanthauza kuti lonjezanolo silowona. Lonjezano la mphamvu ndi mpatso yochokera kwa Mulungu, koma mukuyenera kusakha kulandira mpatso imeneyi.

2. MUKUYENERA KUMVETSA NDONDOMEKO:

Pofuna kutenga lonjezano linalirironse la m’Baibulo, mukuyenera kumvetsa bwino ndondomeko zomwe lonjezanolo laikidwapo. Malonjezano a Mulungu nthawi zonse amakhala pa ndondomeko zomwe amafuna kuti munthu achitepo kanthu. Mwachitsanzo, malonjezano ambiri a Mulungu amakhala pa “ngati/kenako”ndondomeko. “Ngati uchita chinthu china kenako uzalandira lonjezano”. (Onani Deutoronome 20 monga chitsanzo cha ndondomeko imeneyi)

Pofuna kukumana ndi lonjezano la mphamvu ya Uzimu, mukuyenera kulimvetsa bwino Baibulo pa ndondomeko yaza mphamvu. Kudziko la kunthupi, ndizofanana pokuwerenga kaye malangizo amene amabwera ndi chinthu kuti tiphunzire kagwiritsidwe ntchito kwake kapena kuwerenga mmene tingasakanizire zinthu pofuna kuphika zakudya.

3. MUKUYENERA KUGWIRITSA NTCHITO NDONDOMEKO:

Ukapatsidwa mpatso yabwino kwambiri kudziko lakuthupi, mpatsoyi imabwera ndimalangizo amene amayera kuwamvetsa bwino lomwe. Koma ngati usankha kusagwiritsa ntchito malangizo amene ungagwiritsire ntchito ndekuti mpatsoyo izakhala yopanda mphindu kwa iwe.

Okhulupirira wamba sawona mphamvu chifukwa sapitirira mulingo wa madalitso a uzimu. Mzimu Woyera amayamba kuyenda mwa iwo ndipo amakhala ndi chimwemwe chachikulu. Akhoza kuwonetsera izi pakuimba, kukuwa, kuvina, kapenaso kulira. Iwo amakhala kuti adalitsidwa ndi Mulungu ndipo amawonetsera ndi machitachita.

Palibe cholakwika ndizimenezi. Baibulo ndilodzadza ndi machitachita omwe Mzimu amachita. Koma Mulungu amafuna kuuwasutha anthu Ake kuchoka pa mulingo ongodalitsika kufika pamulingo wa mphamvu ya Uzimu, kupitirira pamulingo ongoziwonetsera pamachitachita.

Mu Chipangono Chakale muli nkhani imene imawonetsera choonadi chimenechi.

Imawonetseranso kugwirizana kwa pakati pa lonjezano ndi kutenga kwa lonjezolo. Fuko la Israeli linayenda kwa miyezi yambiri kuchokera kwa Aigupto kudutsa mchipululu kupita ku dziko lomwe Mulungu anawalonjeza. Pamene anafika pafupi ndi dziko lamalonjezano, Mose anatumumiza azondi kuti akazonde dzikolo. Khumi mwa azondiwo anabweretsa uthenga olakwika. Anati kumeneko kuli anthu ataliatali amphamvu ndipo ndi zosatheka kuti tingakatenge dzikolo. Koma awiri okha mwa azondiwo anawalimbikitsa anthu zokalowa ndikutenga dzikolo monga momwe Mulungu anawalonjezera.

Israeli anasakha kumvera uthenga olakwikawo, chifukwa chaichi, ngakhale kuti unali ulendo woyenda masiku khumi ndi limodzi, zinawategera zaka makumi anai kuti akafike ku dziko lamalonjezano (Deutotome 1:2).

Mulungu anafikitsa Israeli pafupi ndi mdalitso. Mphamvu ya Mulungu inalipo kuti igonjetse mphamvu za mdani. Koma Israeli anakana kuti sapita chitsogolo mu mphamvu ya Mulungu. Panalibe cholakwika chirichonse ndi lonjezanolo. Koma vuto linali kukana kwa Israeli kuti akatenge lonjezanolo.

Simukuyenera kuima pamene mwafika pa mdalitso wa moyo wanu. Mukuyenera kubowoleza kufika ku mphamvu ya Uzimu. Ngati simungachite choncho, mupitirizabe kumangozungulira mu mchipululu chouma cha uzimu, chokhala chopanda mphamvu.

Mukuyenera kuyenda kupitirira mulingo wa mdalitso kukafika ku mulingo wa mphamvu.

Mukuyera kukhala woonetsa m'malo mokhala wowonerera, ochita m'malo mwa ongomva.

Pamene muchita choncho, muzamva kuyenda kweni kweni kwa mphamvu ya Mulungu.

Munzamva mphamvu ndikudzodza mwainu zomwe sizinakuchitikirenipo. Muzakhala ndi moyo kupitirira chipembedzo.

ANTHU WAMBA

Mukhoza kumaganiza kuti simungakumane ndi mphamvu imeneyi chifukwa ndinu osaphunzira.

Kapena chifukwa mulibe zoyenerereza kukhala mtumiki ndi tchalitchi. Mukhoza kumakhala kumudzi kutali kwambiri ndi kusukulu yaukachenjede ya Chikhrisitu ndipo mukulephera kuti mukaphunzire maphunziro a Baibulo. Zinthu zonsezi sizofunika kuti mulandire mphamvu ya

Uzimu. Mau a Mulungu adzadza ndi zitsanzo za amuna ndi akazi wamba amene anagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu munjira yamphamvu.

Abrahamu... ananama kuti Sara simkazi wake chifukwa chamatha, koma anagwiritsidwabe ntchito ndi Mulungu kuti apeze fuko lopambana la Israeli.

Mose... anali wosatha kuyakhula ndipo anapha muigupto atakwiya, koma Mulungu anamugwiritsa ntchito kutsogolera mfuko lonse la Israelo.

Petro... amkamira pamene amkayenda panyanja, nthawi zonse amkanena zinthu panthawi yolakwika, mpakana kumapeto kwake anamukana Yesu... koma msodzi uyu anaimirira mkulalikira uthenga wa mphamvu pa tsiku la Pentekoste omwe unapulumsa anthu zikwi zitatu.

Gideon... munthu wang'ono yemwe anabisala kuwopa anthu ozawalanda tirigu koma anaitanidwa kuti azathandize kumasula mfuko lonse mmanja mwa openderezawo.

Mfumu Davide... anapanga chigololo, anatenga mkazi wa mwini ndikumuphaso mamuna wake, koma anali mfumu yopambana ya Israeli ndipo anatchulidwa kuti wake wapamtima wa Mulungu.

Petro ndi Yohane... osewa anali asodzi osauka ndipo analibe ndalama zolipirira maphunziro awo, koma mphamvu yochiza ya Mulungu inali mwa iwo yomwe inagwedeza mzinda onse.

Mtumwi Paulo... zinatedwa za iye kuti makalata ake anali olemera ndi amphamvu, koma maonekedwe athupi lake anali ofooka komaso mau ake ngachabe (2 Akorinto 10:10)

Yakobo... anali wonama, wachinyengo ndiposo wakuba. Koma pamene Mulungu anamukhudza, anakhala “kalonga wa mphamvu kwa Mulungu ndi munthu.”

Ngati anthu awa angakhulupiriribe ndi mphamvu ya Uzimu ndi Mulungu komaso anthu, ndekuti inuso muntha kukhulupiridwa, posayang'anira zolephera zanu! Mulungu amaitana amuna ndi akazi wamba ndikuwapanga kukhala apamwamba. Samakuwonani ngati mmene inu maziwonera nokha. Samakuwonani ngati momwe ena amakuwonerani. Mulungu amakuwonani chomwe mungakhale ngati mutapatsidwa mphamvu ya Uzimu. Mulungu amagwiritsa ntchito anthu wamba, zimene Baibuli limati “chotengera chadothi” kuti...”**ukulu wopasa wamphamvu ukhale wa Mulungu, osachokera kwa ife.**” (2 Akorinto 4:7)

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera ya muchaputala ichi.

2. Kodi pali kusiyana kotani pakati pa chipembedzo ndi kuwonetsera mphamvu ya Mulungu?

3. Tchulani ndondomeko zina za mphamvu ya kudziko zomwe zalembedwa muphunziroli.

4. Kodi ndi umboni uti umene ukufotokoza kusiyana pakati pamndandanda wa mphamvu za ku dziko lakuthupi ndi mphamvu za m’Baibulo?

5. Perekani tanthauzo la mphamvu ndi ulamuliro malingana ndi Baibulo.

6. Wonetsani gwero lopera chilengedwe lomwe ndi gwero la mphamvu ya Uzimu.

7. Kodi ndi mbali ziwiri ziti za malonjezano a m’Baibulo?

_____ ndi _____

8. Lembani ndondomeko zitatu zomwe zaperekedwa mu phunziroli zotengera malonjezano a Mulungu.

9. Maziko a mphamvu ya Uzimu ndi_____.

(Mayankho amayesowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Kulemba koyamba kwa Baibulo kwa munthu kuti anadzazidwa ndi mphamvu ya mzimu ndi Yakobo. Zinalembedwa za iye kuti anali ndi mphamvu ya Mulungu ndi munthu. Phunzirani za izi mu Genesis 32 ndi Hoseya 12:3-4. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira pa ndime zimenezi:

2. Yesu anakana mphamvu za dziko lapansi. Onani Luka 4:1-13, Yohane 6:15, ndi Yohane 7:2-6. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira pandime imenewyi.

CHAPUTALA 2

KOCHOKERA MPHAMVU

ZOLINGA:

Pomapeto pa phunziro ili muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Kuwonetsa komwe mphamvu zimachokera.
- Kulemba njira zisanu ndi zitatu momwe Mulungu anawonetsera mphamvu zake pa dziko lapansi.
- Kupereka umboni wa mmalemba omwe umafotokoza chifukwa chomwe Mulungu anawonetsera mphamvu Zake pa dziko lapansi.

VESI YOTSOGOLERA:

Mulungu ananena kamodzi, ndinachimva kawiri: kuti mphamvu ndi yake ya Mulungu. (Masalimo 62:11).

MAU OYAMBA

Kuti timvetse bwino pa zandondomeko za mphamvu tikuyenera kuyambira pachiyambi penipeni. Tikuyenera kuzindikira kumene mphamvu zimachokera. Gwero lachinthu ndi chiyambi chake kapena malo omwe chimayambira. Chaputala ichi chiwonetsera Mulungu wowona komaso wamoyo monga mmene Baibulo lawonetsera kuti Iye ndi chiyambi champhamvu zonse. Davide analemba:

Mulungu ananena kamodzi, ndinacimva kawiri: Kuti mphamvu ndi yace ya Mulungu: (Masalimo 62:11)

Pamene Mulungu akubwereza chinthu ndekuti chinthucho ndichofunika kwambiri.

KOCHOKERA MPHAMVU

China chirichonse chisanakhalepo, panali Mulungu yekha. Genesis 1-2 amakamba zachiyambi chadziko. Mulungu analenga dziko lapansi ndi mpamvu Zake.

Iye analenga dziko lapansi ndi mphamvu yace, nakhazikitsa dziko lapansi ndi nzeru yace, nayala thambo ndi kuzindikira kwace; (Yeremiya 10:12)

Ine ndinalenga dziko lapansi, anthu ndi nyama zokhala m'dzikomo, ndi mphamvu yanga yaikuru ndi mkono wanga wotambasuka; ndipo ndinapereka ilo kwa iye amene ayenera pamaso panga. (Yeremiya 27:5)

pakuti mwa iye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando yacifumu, kapena maufumu, kapena maukulu, kapena maulamuliro; zinthu zonse zinalengedwa mwa iye ndi kwa iye. (Akolose 1:16)

Pakuti Mulungu analenga zinthu zonse, nde palibe chopitirira mphamvu Yake:

Ha! Yehova Mulungu, taonani, Inu munalenga kumwamba ndi dziko lapansi ndi mphamvu yanu yaikuru ndi mkono wanu wotambasuka; palibe cokulakani Inu; (Yeremiya 32:17)

Mulungu nde kochokera mphamvu yachina chirichonse mmene chiriri pano:

Ndipo pozinga mpando yacifumu mipando yacifumu makumi awiri mphambu inai; ndipo pa mipandoyo padakhala akuru makumi awiri mphambu anai, atabvala zobvala zoyera, ndi pamitu pao akorona agolidi. (Chibvumbulutso 4:11)

Cifukwa 7 zinthu zonse zicokera kwa iye, zicitika mwa iye, ndi kufikira kwa iye. 8 Kwa Iyeyo ukhale ulemerero ku nthawi zonse. Amen. (Aroma 11:36)

ameneyo, pokhala ali cinyezimiro ca ulemerero wace, ndi cizindikilo ceni ceni ca cikhalidwe cace, nanyamula zonse ndi mau a mphamvu yace, m'mene adacita ciyeretso ca zoipa, anakhala pa dzanja lamanja la Ukulu m'Mwamba, (Ahebri 1:3)

Mulungu ali ndi nthawi ndi nyengo mu mphamvu Zake:

Koma anati kwa iwo, Sikuli kwa inu kudziwa nthawi kapena nyengo, zimene Atate anaziika m'ulamuliro wace wa iye yekha. (Machitidwe 1:7)

Dziko lapansi ndizonse zokhalamo ndi za Mulungu:

Dziko lapansi nla Yehova ndi zodzala zace zomwe, Dziko lokhalamo anthu ndi iwo okhala m'mwemo. (Salimo 24:1)

Mu Genesis 14: 22, Mulungu akutchulidwa kuti Mwini kumwamba ndi dziko lapansi. Kukhala mwini wa chinthu zikutanthauza kuti uli ndi mphamvu pachimenecho.

Pali ma ufumu ndi maboma mu dziko lino. Koma ufumu wa Mulungu ndi wamuyaya.

Izi zikutanthauza kuti Iye amalamulira china chirichonse

Yehova anakhazika mpando wacifumu wace Kumwamba; Ndi ufumu wace ucita mphamvu ponsepo, (Salimo 103:19)

Ukulu, ndi mphamvu, ndi ulemerero, ndi kulakika, ndi cifumu ndi zanu, Yehova; pakuti zonse zam'mwamba ndi pa dziko lapansi ndi zanu; ufumu ndi wanu, Yehova; ndipo mwakwezeka mutu wa pa zonse. Zolemera ndi ulemu zifuma kwanu, ndipo mucita ufumu pa zonse, ndi m'dzanja mwanu muli mphamvu yaikuru; kukuza ndi kupatsa onse mphamvu kuli m'dzanja lanu. (1 Mbiri 29:11-12)

Pakuti Mulungu analenga munthu, ndekuti ali ndi ulamuliro pa mzimu wanthuyo:

Kulibe munthu ali ndi mphamvu yolamulira mzimu ndi yakutsekereza mzimu; ngakhale mphamvu tsiku la imfa; munkhondo umo mulibe kumasuka; udio sudzapulumutsa akuzolowerana nao. (Mlaliki 8:8)

Mulungu ali ndi mphamvu zoteteza onse amene asakhidwa kuti afe:

Kubuula kwa wandende kufike kuli Inu; Monga mwa mphamvu yanu yaikuru lolani ana a imfa atsale; (Masalimo 79:11)

Mulungu ndi amene amapereka mphamvu kwa okomoka:

Iye alimbitsa olefuka, naonjezera mphamvu iye amene alibe mphamvu. (Yesaya 40:29)

Inu Mulungu, ndinu woopsa m'malo oyera anu; Mulungu wa Israyeli ndiye amene apatsa anthu ace mphamvu ndi cilimbiko. Alemekizeke Mulungu. (Masalimo 68:35)

Mphamvu za Mulungu sizisokonezedwa ndi mphamvu kapena kusowa mphamvu kwa munthu:

Ndipo Asa anapfuulira kwa Yehova Mulungu wace, nati, Yehova, palibe wina ngati Inu, kuthandiza pakati pa wamphamvu ndi iye wopanda mphamvu; tithandizeni Yehova Mulungu wathu, titama Inu, taturukira aunyinji awa m'dzina lanu. Yehova, Inu ndinu Mulungu wathu, munthu asakulakeni. (2 Mbiri 14:11)

Mulungu ali ndi mphamvu zopulumutsa. Baibulo ladzadza ndi zitsazno za zomwe Mulungu anapulumutsira anthu munthawi zosowa. Zitsanzo ziwiri zabwino zikupezeka mu buku la Daniele. Werengani mmene Mulungu analanditsira atumiki Ake mu ng'anjo ya moto ndi mu dzenje lamikango mu Daniele 6.

Mphamvu zake ndizopanda malire:

Yehova ndiye wolekerera mkwiyo, koma wa mphamvu yaikuru; ndi wosamasula ndithu woparamula; njira ya Yehova iri m'kabvumvulu ndi mumkuntho; ndipo mitambo ndiyo pfumbi la mapazi ace. (Nahumu 1:3)

Mphamvu zake ndi zoposa:

Kunena za Wamphamvuyonse, sitingamsanthule; ndiye wa mphamvu yoposa; Koma mwa ciweruzo ndi cilungamo cocuruka samasautsa. (Yobu 37:23)

Mphamvu za Mulungu ndi zamuyaya. Paulo analemba kuti Mulungu:

amene iye yekha ali nao moyo wosatha, wakukhala m'kuunika kosakhozeka kufikako; amene munthu sanamuona, kapena sakhoza kumuona; kwa iye kukhale ulemu ndi mphamvu yosatha. Amen. (1 Timoteo 6:16)

Mu buku lomaliza la m'Baibulo timawerenga zomwe zizachitike kumwamba mtsogolomu...

Ndipo Kacisi anadzazidwa ndi utsi wocokera ku ulemerero wa Mulungu ndi ku mphamvu yace; ndipo palibe munthu anakhoza kulowa m'Kacisi kufikira ikatha miliri isanu ndi iwiri ya angelo asanu ndi awiri. (Chibvumbulutso 15:8)

kunena, Amen: Thamo ndi ulemerero, ndi nzeru, ndi ciyamiko, ndi ulemu, ndi cilimbiko, ndi mphamvu zikhale kwa Mulungu wathu kufikira nthawi za nthawi. Amen. (Chibvumbulutso 7:12)

Zitatha izi ndinamva ngati a mau akuru khamu lalikuru m'Mwamba, liri kunena, Aleluya; cipulumutso, ndi ulemerero, ndi mphamvu, nza Mulungu wathu; (Chibvumbulutso 19:1)

Mobwerezabwereza, kuyambira pachiyambi kukafika kumapeto, Baibulo liamanena kuti Mulungu nde kochokera mphamvu.

MMENE MULUNGU ANAWONETSERA MPHAMVU ZAKE.

Baibulo linalamba mmene Mulungu anawonetsera mphamvu zake pa dziko lapansi. Izi ndi njira zosiyasiyana zomwe Mulungu anawonetsera mphamvu zake:

CHILENGEDWE:

Mulungu waziwonetsera yekha muchilengedwe. Zomera ndi zinyama, zigwa ndi mapiri, madzi ndi zipululu, ngakhale miyamba ndizizindikiro zooneka zamphamvu yake yolenga:

Haleluya, Lemekezani Mulungu m'malo ace oyera; Mlemekezeni m'thambo la mphamvu yace. (Masalimo 150:1)

Ndinu amene mukhazikitsa mapiri ndi mphamvu yanu; Pozingidwa naco cilimbiko. Amene atontholetsa kukuntha kwa nyanja, kukuntha kwa mafunde ace, Ndi phokoso la mitundu ya anthu. (Masalimo 65:6-7)

Mulungu ali mumphepo, Nyanja, ndi mapiri:

Anaombetsa m'mwamba mphepo ya kum'mawa: Natsogoza mwela ndi mphamvu yace. (Masalimo 78:26)

Yehova ndiye wolekerera mkwiyo, koma wa mphamvu yaikuru; ndi wosamasula ndithu woparamula; njira ya Yehova iri m'kabvumvulu ndi mumkuntho; ndipo mitambo ndiyo pfumbi la mapazi ace. Adzudzula nyanja, naiphwetsa, naumitsa mitsinje yonse; Basana ndi Karimeli afota, ndi duwa la ku Lebano linyala. Mapiri agwedezeke cifukwa ca Iye, ndi zitunda zisungunuka; ndi dziko lapansi likwezeke pamaso pace, ndi maiko ndi onse okhala m'mwemo. (Nahumu 1:3-5)

Amalamulira zonse zopezeka muchilengedwe:

polankhula Iye, pali unyinji wa madzi m'mwamba, ndipo akweretsa nkhungu ku malekezero a dziko lapansi, alenga mphezi idzetse mvula, naturutsa mphepo m'zosungira zace. (Yeremiya 10:13)

Yobu chaputala 38-40 imapereka mndandanda wazolemba momwe Mulungu waziwonetsera mudziko lakuthupi. Mulungu wawonetsera mphamvu zake za bwino muchilengedwe zomwe zimapangitsa munthu kuti asakhale zifukwa posakhulupirira Mulungu:

Pakuti cilengedwere dziko lapansi zaoneka bwino zosaoneka zace ndizo mphamvu yace yosatha ndi umulungu wace; popeza zazindikirika ndi zinthu zolengedwa, kuti iwo adzakhale opanda mau akuwiringula; (Aroma 1:20)

MAU AKE OLEMBEDWA:

Kuyambira pachiyambi mpakana kumapeto, mau olembedwa a Mulungu amawonetsera mphamvu Yake. Amayamba ndi mphamvu yake yolenga. Limalamaliza ndi mphamvu Yake yowononga, kuweruza, ndikuzalenganso. Pakati pa Genesis ndi Chibvumbulutso, mau a Mulungu analemba zamphamvu yake ili kuchitachita mudziko ndi miyoyo ya amuna ndi akazi.

Nkhani zolembedwazi sizimangowonetsera mphamvu ya Mulungu, komaso kuti mau amene anayakhula ndi amphamvu:

Pakuti mau a Mulungu ali amoyo, ndi ocitacita, ndi akuthwa koposa lupanga lakuthwa konse konse, napyoza kufikira kugawira moyo ndi mzimu, ndi zimfundo ndi mafuta a m'mafupa, nazindikiritsa zolingirira ndi zitsimikizo za mtima. (Ahebri 4:12)

CHIWERUZO:

Mchitidwe wa chiweruzo cha Mulungu umawonetsera mpamvu Yake. Mphamvu zake koyambirira zinawonetsedwa muchiweruzo pamene anamuluza Adamu ndi Hava chifukwa cha tchimo lawo (Genesis 3).

Zinawonetsedwera kwambiri pamene Mulungu anawononga dziko lonse ndi madzi muthawi ya Nowa (Genesis 6-9).

Baibulo ndi mndandanda wazolemba zomwe zimapitiriza kuwonetserabe mphamvu ya Mulungu pakudzera pakuweruza tchimo. Amatumiza chiweruzo kwa anthu ake pamene achimwa.

Amatumizaso chiweruzo kwa maiko amene akuchita zoipa. Mukhoza kuwerenga izi mu buku la Oweruza ndi ma buku olembedwa ndi aneneri.

Nthawi iriyonse pamene Mulungu watumiza chiweruzo, Amanene mwachindunji kuti amafuna anthu kuti adziwe za mphamvu Yake (Mwachitsanzo, onani Eksodo 7:17)

CHIOMBOLO:

Kupyolera mu mbiri, Mulungu wawonetsera mphamvu Yake munjira yozizwitsa mu kuwombola.

Ngakhale Mulungu anaweruza Adamu ndi Hava , koma anapereka njira yachipilumutso kwa iwo

ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yace; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira citende cace. (Genesis 3:15).

Ngakhale anawononga dziko lapansi loyipa ndi madzi, anapereka chombo chopulumukirapo

Mibadwoya Nowandiiyi: Nowa anali munthu wolungama ndi wangwiro m'mibadwo yace; Nowa anayendabe ndi Mulungu. (Genesis 6-9).

Mulungu anawombola Israeli kuchoka kugoli la ukapolo ku Igupto kupyolera mu mphamvu Yake:

Ndipo popeza anakonda makolo anu, anasankha mbeu zao zakuwatsata, nakaturutsani pamaso pace ndi mphamvu yace yaikuru, m'Aigupto; (Deutoromo 4:37)

Mulungu anadzutsa oweruza, mafumu ndi aneneri amene Anawagwiritsa ntchito kuwombola anthu Ake kuchoka kudzanja la adani. Nehemiya anati za Israeli:

Ndipo awa ndi akapolo anu ndi anthu anu, amene munawaombola ndi mphamvu yanu yaikuru, ndi dzanja lanu lolimba. (Nehemiya 1:10)

Panthawi iriyonse yomwe Mulungu wawombola anthu Ake, amakhala ali ndicholinga. Cholinga chimenecho pakuwonetsera mphamvu Yake:

Koma anawapulumutsa cifukwa ca dzina lace, Kuti adziwitse cimphamvu cace. (Salimo 106:8)

YESU KRISTU:

Ndondomeko ya Mulungu yaikulu yowombola inawonetseredwa mwa Yesu Kristu kupyolera mwa Iye anthu onse akhoza kuombedwa kumachimo ku nthawi zonse.

Mphamvu ya Mulungu inawonetsedwera kudzera mu ma uneneri okhudzana kubadwa kwa Yesu kodabwitsa. Zinawonekera mu moyo, muchiphunzitsa ndi utumiki wa Ambuye ngakhaleso mu imfa ndi kuuka kwake.

Bvumbulutso lalikulu la mphamvu ya Mulungu linali mwa Yesu Kristu:

Ndipo ndinamva mau akuru m'Mwamba, nanena, Tsopano zafika cipulumutso, ndi mphamvu, ndi ufumu za Mulungu wathu, ndi ulamuliro wa Kristu wace; pakuti wagwetsedwa wonenera wa abale athu, wakuwanenera pamaso pa Mulungu wathu usana ndi usiku. (Chibvumbulutso 12:10)

MZIMU WOYERA:

Yesu analonjeza ophunzira Ake:

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko. (Machitidwe 1:8)

Machitidwe 2 imakamba za kubwera kwa Mzimu Woyera, wotumizidwa kuchokera kwa Mulungu monga momwe Yesu analonjezera. Mwakubwera kwa Mzimu Woyera Mulungu akupitirizabe kuwonetsera mphamvu Yake. Muzazindikira pamene muzaphunzira zamphamvu ya Mzimu Woyera kutsogolo kwa phunziro lino.

ZIZINDIKIRO ZAUZIMU:

Mwaphunzira kale kuti Mulungu amawonetsera mpamvu zake kudzera mu chiweruzo ndi chiwombolo kwa anthu Ake. Komaso Mulungu amawonetsera mphamvu zake kudzera mu njira zauzimu. Kuposa chilengedwe zimatanthauza kuti kuposera mphamvu ya dziko zakuthupi. Ndi zinthu zakuti sizingapangidwe ndi mphamvu za munthu.

Mphamvu ya Mulungu inawonetseredwa kudzera mmachiritso ozizwitsa, kumasulidwa kumphamvu ya ziwanda, kubwezeretsaso moyo kwa akufa ngakhaleso moyo kutsika kuchokera kumwamba. Baibulo lonse linadzadza ndi zizindikiro zamphamvu kuposa mphamvu zadziko

lapansi. Mphamvu ya Mulungu ikuwonekerabe kudzera mu zizindikiro zimemenezo mpakana lero.

OKHULUPIRIRA:

Yesu anati zizindikiro za mphamvu zizachitidwa ndi Mulungu kudzera mwa okhulupirira:

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Marko 16:17-18)

Kuyambira pachiyambi pa mau Ake olembedwa, Mulungu wakhala akugwira ntchito kudzera mwa amuna ndi akazi padziko lapansi. Munthu ali ndi kuthekera kokhala ndi mphamvu kuposera cholengedwa china chilochonse. Chiweruzo cha Mulungu chinabwera chifukwa cha uchimo omwe amuna ndi akazi anachita. Chiombolo chinabwera kupyolera mwa olungama oweruza, aneneri, mafumu, kenako kupyoleraso mwa Yesu Kristu.

Pamene Yesu anabwera pa dziko lapansi kuzawonetsera mphamvu za Mulungu, anababwa kudzera kwa mkazi mwa umunthu. Chiwombolo chachikulu ku nthawi zonse, chiwombolo cha machimo, chinabwera kudzera mwawina yemwe anapangidwa monga munthu.

Pamene Yesu anabwelera kupita kumwamba, Mulungu anapitirizabe kuwonetserabe mphamvu zake pano dziko lapansi kupyolera mwa amuna ndi akazi. Buku la Machitidwe linalimba za mphamvu ya Mulungu yomwe imkagwira ntchito kupyolera mwa okhulupirira.

Ndipo iwowa anaturuka, nalalikira ponse ponse, ndipo Ambuye anacita nao pamodzi, natsimikiza mau ndi zizindikilo zakutsatapo, Amen. (Marko 16:20)

Mphamvu ya Mulungu inawonekera kudzera mu mphamvu ya uthenga wabwino yomwe inasitha miyoyo ya amuna ndi akazi. Inawonekera kupyolera pakuchilitsa ndi kumasula mozizwitsa.

Mphamvu yake inawokerabe ngakhale mkatikati mwamazuzo.

Pamene Mulungu akudzutsa munthu kapena utumiki akhala ndi cholinga chakuti awonetsera mphamvu Zake. Mulungu anati kwa Mose:

Koma ndithu cifukwa cace ndakuimika kuti ndikuonetse mphamvu yanga, ndi kuti alalikire dzina langa pa dziko lonse lapansi. (Eksodo 9:16)

Mulungu akupitirizabe kuwonetsera mphamvu Yake lero kupyolera mwa okhulupirira amene ali mbali imodzi ya mpingo weniweni. Amawonetsera mphamvu yake kupyolera mwa atsogoleri apaderadera omwe amapatulidwa mu mpingo komaso kudzera mu mphatso za uzimu zomwe zimaperkedwa kwa okhulupirira. Muphuzira za izi mu chaputala 5 paza “kupatsidwa ulamuliro”.

NCHIFUKWA CHIANI MULUNGU AMAWONETSERA MPHAMVU ZAKE?

Nchifukwa chiani Mulungu amawonetsera mphamvu zake padziko lapansi? Nchifukwa chani amawonetsera zizindikiro za zozizwa kwa munthu? Muphunzira za izi mu chaputala 6 “cholinga cha mphamvu.”

Koma zolinga za mphamvu ya Mulungu zikhoza kunenedwa mucholinga chimodzi chachikulu. Cholinga ichi kuyambira pachiyambi cha nthawi, chinali kuwombola munthu wochimwa kupyolera mwa Yesu Kristu. Cholinga chobvumbulutsira mphamvu yake ndichofuna kuwasendezera anthu kwa Iye kudzera mwa Yesu.

Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:9-10)

monga mwa citsimikizo mtima ca nthawi za nthawi, cimene anacita mwa Kristu Yesu Ambuye wathu: (Aefeso 3:11)

MULINGO WINA WA ULAMULIRO

Mulungu nde gwero la mphamvu zonse. Ali pamwamba komaso ali ndi ulamuliro padziko lonse.

Mulungu wakhazikitsa milingo ina ya ulamuliro padziko. Anapereka ulamuliro kwa Mwana wake, Yesu Kristu. Amaperekaso ulamuliro kwa okhulupirira kupyoleramwa Mzimu Woyera. Mulungu wakhazikitsa milingo ya ulamuliro mdera, m'boma, muzamalonda, makomo komaso makachisi. Milingo ya ulamuliro yonseyi ndi yofunika. Kuti mumvetse bwino ndondomeko ya zamphamvu ya uzimu, mukuyenera kuzindikira mndandanda wa ulamuliro omwe Mulungu akhazikitsa. Muphunzira za izi kutsogoloku.

Koma choyamba, chidwi chikuyenera kuikidwa pa pa choonadi chomwe chaululidwa mu Baibulo. Ngakhale Mulungu ndi gwero la mphamvu, sizikutanthauza kuti ulamuliro wake sumatsutsidwa. Kuli mphamvu za woipa zomwe zimatsutsa ulamuliro wa Mulungu. Koma ichi

sichiopsyezo ku ulamuliro wake munjira iliyonse, koma nthawi zonse zimakhala zikumenya nkhondo. Ngati mungabweretse “ndondomeko za mphamvu” miyoyo yanu monga mmene Baibulo likunenera, muzakumana ndi zotsutsa zambiri kuchokera kumphamvu za oipa. Chaputala chotsatira “kulimbana ndi chinyengo” chikikufotokoza za mutu umenewu.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yapamtima yoloweza.

2. Kodi chiyambi chachinthu nchani?

3. Kodi ndindani amene ali gwero la mphamvu zonse?

4. Lembani njira zisanu ndi zitatu zomwe Mulungu amawonetsera mphamvu Zake pano padziko.

5. Kodi izi ndizowona kapena zonama? “Mulungu ndi mphamvu yokhayo mudziko lonse. Palibeso milingo ina ya mphamvu.” Kunena uku ndi_____.

6. Perekana malemba omwe amafotokoza cholinga chenicheni chomwe Mulungu amawonetsera mphamvu Yake padziko lapansi.

(Mayakho amayesowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli.)

ZOONJRZERA POPHUNZIRA

1. Davide anali mfumu yopambana yomwe inalamulira dziko la Isreali. Anazindikira Mulungu ngati chiyambi cha mphamvu zonse. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira kuchokera kuma vesi awa:

2 Samueli 22:33; Salimo 59:11,16; 62:2; 65:6; 68:35; 78:26; 79:11; 90:11; 106:8; 110:3; 111:6; 145:11; 150:1

2. Davide awonetsera zokhumba za umunthu zomwe zinali zogwirizana ndi mphamvu ya Mulungu. Kodi chinali chokhumba chanji chomwe chinawonetseredwa mu Salimo 71:18?

3. Pamene mukuphunzira Baibulo, muzisunga mmene Mulungu waonetsera mphamvu Yake kupyolera:

Chilengedwe

Yesu Kristu

Chiweruzo

Mzimu Woyera

Chiwombolo

zizindikiro zoposa mphamvu yachilengedwe

Mau Ake olembedwa

Okhulupirira

CHAPUTALA 3

KULIMBANA NDI CHINYENGO

ZOLINGA:

Pomaliza pachaputala ichi mukuyenera kukwanitsa ku:

- Kulemba vesi yoloweza yapamtima.
- Kuwonetsera satana monga okhala ndi mphamvu yachinyengo yolimbana ndi mphamvu yeni yeni ya Mulungu.
- Kufototokoza tanthauzo la “kuipa kwa uzimu malo akuluakulu.”
- Kulemba mwachidule mmene satana amakoperera mphamvu ya Mulungu kudzera kuipa kwa uzimu malo akuluakulu.

VESI YOTSOGOLERA:

Ndipo kulibe kudabwa; pakuti satana yemwe adzaonetsa ngati mngelo wa kuunika. Chifukwa chake sikuli kanthu kwakukulu ngatinso atumiki ake adzionetsetsa monga atumiki a chilungamo; amene chimariziro chao chidzakhala monga ntchito zao.(2 Akorinto 11:14-15)

MAU OYAMBA

Mu chaputala chapita chija mwaphunzira kuti Mulungu ndiye chiyambi cha mphamvu zonse ndipo njira iliyonse amawonetsera mphamvu Yake pano padziko lapansi. Koma mphamvu za Mulunguzi zimatsutsidwa. Pali kulimbirana mphamvu komwe kukuchitika pa dziko. Koma sikuti ndi nkondo ya nthupi kapenaso mwazi. Koma ndikulimbana kwakukulu ndi chinyengo choukira Mulungu.

KULIMBANA NDI ZOKOPERA

Satana kawirikawiri amalimbana ndi mphamvu ya Mulungu mu dziko. Amalimbana popanga zachinyengo koma sapereka chiwopsyezo china chirichonse kwa Mulungu. Satana analengedwa ndi Mulungu monga mngelo wokongola ndipo anampatsa dzina lakuti Lusifala. Werengani chiyambi chenicheni ndi udindo wake mu Ezeieli 28:12-17. Koma satana anaukira mphamvu ndi ulamuliro wa Mulungu. Amkafuna kuti iye akhale Mulungu. Mukhoza kuwerenga nkhani

youkirayi pa Ezeieli 28:17 ndi Yesaya 14:12-15. Mulungu anakatha kumukatha ndi kumupheratu satana chifukwa chakuukira kwakeko. Koma anakathana naye mdani woyamba mwanjira imeneyi ndekuti pakanabweraso mdani wina, kotero nkhani yakumwamba bwezi itangodzadza ndi mbiri zoukira.

Mmalo mwake Mulungu anamuthamangitsa Satana kumwamba ndikumulola kuti akhale padziko lapansi kuti mlandu wake uzaweruzidwe bwino. Mulungu anathamangitsaso angelo ena amene anatenga nawo mbali pakuukira kwa satana. Ena mwa iwo ndi angelo oyipa amene amadziwika kuti “ziwanda” kapena “tiasatana” amene akugwira ntchito lero pa dziko lapansi.

Patangodutsa nthawi yochepa Mulungu atalenga mamuna ndi mkazi woyamba, nkondo inayambika pa dziko lapansi. Timaweranga za kulimbana koyamba mu Genesis chaputala 3. Kugwa kwa Adamu ndi Hava kutchimo kunachokera kukuwukira ulamuliro ndi mphamvu za Mulungu. Adamu ndi Hava amkafuna kuti akhale ndi chidziwitso chofanana ndi Mulungu.

Kuchokera panthawi imeneyi, Satana wakhala akuukira ulamuliro wa Mulungu pano padziko lapansi. Kupyolera mutchimo, satana wakhala akuyesetsa kukopa amuna ndi akazi kuti akhale mbali yake mmalo mokhala mbari ya Mulungu. Phunziro la The Harvest Institute, “*buku la Nkhondo ya uzimu*” limakamba kwambiri pa mutu wa satana mwatsatanetsatane. Ngati mukuphunzira maphunzirowa mundondomeko imene inakhazikitsidwa, ndekuti munaphunzira kale phunziro limeneri. Ngati ndi ayi, tikukupephani kuti mulipeze kuti mumvetse bwino za mdani ameneyu ndikutiso mudziwe ndondomeko za uzimu zomwe mungagwiritse ntchito kuti mupambane mphamvu yake.

Njira imodzi yayikulu yomwe satana magwiritsa ntchito powukira mphamvu ya Mulungu nde ndikupanga mphamvu za chinyengo. Kukopera ndi kutsanzira kwa chinthu china chake ndipo chimapangidwa kuti chikanyenge. Mwachitsanzo, ndalama zachinyengo zimapangidwa kuti ziwoneke ngati ndalama zenizeni. Mbava zimapereka ndalamazi kwa ena ngati ndalama zenizeni ndi cholinga chowanamiza.

Satana anakopera mphamvu ya Mulungu. Amatsanzira mphamvu ya Mulungu kuti anamize anthu. Amagwiritsa ntchito angelo(ziwanda) ake kuti amuthandizire kuti akwaniritse cholinga chake. Satana ndi ziwanda zake nthawi zina amaoneka ngati abwino osati oyipa.

Tikuchenjezedwa:

Ndipo kulibe kudabwa; pakuti Satana yemwe adzionetsa ngati mngelo wa kuunika. Cifukwa cace sikuli kanthu kwakukuru ngatinso atumiki ace adzionetsa monga atumiki a cilungamo; amene cimariziro cao cidzakhala monga nchito zao. (2Akorinto 11:14-15)

Masiku omaliza pa dziko lapansi, kukopera kwa mphamvu ya Mulungu ndi satana kuzachulukira. Kupyolera mu zozizwa ndi zizindikiro, azanyenga ambiri:

ndiye amene kudza kwace kuli monga mwa macitidwe a Satana, mu mphamvu yonse, ndi zizindikilo ndi zozizwa zonama; ndi m'cinyengo conse ca cosalungama kwa iwo akuonongeka, popeza cikondi ca coonadi sanacisandira, kuti akapulumsidwe iwo. Ndipo cifukwa cace Mulungu atumiza kwa iwo macitidwe a kusoceretsa, kuti akhulupirire bodza; (2 Aterosanika 2:9-11)

Malemba awa akuwonetsera mmene satana amagwirira ntchito. Amakopera mphamvu ya Mulungu ndi “mphamvu zonse, zizindikiro ndi zozizwa zabodza.” Njira yokhayo imene mugathe kuzindikira chinyengo chakechi ndikudzera mu mau owona a Mulungu basi.

MAULAMULIRO NDI MPHAMVU

Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:12)

Munthu wakodwa mumkangano wa satana owukira mphamvu ya Mulungu. Talowa nawo mukulimbirana mphamvu kupyolera mu mphamvu zasatana zosawoneka. Koma mphamvu ya Mulungu ndiyoposa “mipando ya chifumu, maufumu, maukulu, maulamuliro ndi mphamvu” (Akolose 1:16) ndipo ndi wopambana kwambiri kuposera “maulamuliro ndi mpamvu m'zakumwamba” (Aefeso 6:12). Koma mukuyenera kukhala tcheru kumphamvu yachinyengo ya satana yomwe amakopera mphamvu ya Mulungu. Mukuyenera kukhala ozindikira pa...

ZOIPA ZA UZIMU MMIYAMBA

Pamene Paulo amkayakhula za “zoipa za uzimu mmiyamba,” amakamba za mizimu yoipa yomwe yalowerera mu chipembedzo cha dziko lapansi. Satana wasokhanitsa mphamvu zake zoipa kuti akakopere mpingo weni weni wa Mulungu, mu nthawi zina amakhala ndi mipingo

yomwe imadziwika kuti “mpingo wa satana” kapena “auzimu”. Anakhazikitsa ndondomeko yakalambiridwe mu uzimu “mmiyamba” mumsokhano wa chipembedzo.

Satana wakhazikitsaso ndondomeko yake mu mpingo kupyolera kwa anthu akuchita zoipa amene “akwawira m’seri” (Yuda 4). Satana ali tchalitchi kuwonetsera mphamvu, koma izi simphamvu za Mulungu. Ndongomeko zomwe Satana wakhazikitsa pamwamba pa chipembedzo wakhazikika kwambiri pokopa ndi kunyenga basi.

SATANA ALI NAWO UTATU WAKE:

Mulungu ndi utatu wa Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Utatu wa satana uli ndi satana iye mwini, chilombo, ndi aneneri onyenga.

SATANA ALI NDI MPINGO WAKE:

Mulungu anakhazikitsa mpingo wake umene umadziwika kuti “Nthupi la Kristu” omwe mutu wake ndi Yesu:

Akorinto 12:27 Koma inundinu thupi la Kristu, ndi ziwalo, yense pa yekha. (1 Akorinto 12:27)

Satana naye alinawo mpingo wake ndipo umatchulidwa kuti “sunagoge wa satana”

Ndidziwa cisautso cako, ndi umphawi wako (komatu uli wacuma), ndi mwano wa iwo akunena za iwo okha kuti ali Ayuda, osakhala Ayuda, komatu sunagoge wa Satana. (Chibvumbulutso 2:9)

Dzina lakuti “sunagoge wa satana” siligwiritsidwa ntchito mowonetsera, koma sunagoge ameneyu amakhazikitsidwa pali ponse pomwe Uthenga wabwino wa Ambuye Yesu Kristu sunalalikidwepo.

SATANA ALI NDI ZIPHUNZITSO:

Mulungu ali ndi ziphunzitso zomwe zawonekera mu Mau ake oyera, Baibulo:

Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitso, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: (2 Timoteo 3:16)

Chiphunzitso cha satana chimatchulidwa kuti “chiphunzitso chaziwanda”

Koma Mzimu anena monenetsa, kuti m' masiku otsiriza ena adzataya cikhulupiriro, ndi kusamala mizimu yosoceretsa ndi maphunziro a ziwanda, (1 Timoteo 4:1)

Chiphunzitso chaziwanda ndi chiphunzitso chirichonse chimene chimabwera ngati choona koma sichigwirizana ndi mau a Mulungu.

SATANA ALI NDI MCHITIDWE OPEREKA MSEMBE:

Mu Aroma 12:1, timauzidwa kuti tizipereke tokha kwa Mulungu monga msembe yamoyo. Izi zikutanthauza kuti tikuyenera kuzipereka kwanthunthu kwa Mulungu. Naye satana amafuana msembe:

Koma nditi kuti zimene amitundu apereka nsembe azipereka kwa ziwanda; ndipo sindifuna kuti inu muyanjane ndi ziwanda. (1 Akorinto 10:20)

Satana amafuna kuzipekereka kwathuthu kwa moyo, nthupi ndi mzimu. Pamakhala kupereka msembe yeni yeni pamene amuna ndi akazi akuzipereka ku ntchito ya satana. Msembe ya mwazi wa anthu kapena nyama imaperekedwa.

SATANA ALI NDI MGONERO WAKE:

Kugawana kwa mkate pa mgonero ndi kumwa chikho zinayamba ndi Yesu monga ngati njira yokumbukira msembe yomwe anapera chifukwa chamachimo a anthu pa mtanda (1 Akorinto 11:23-34). Satana anakopera izi:

Simungathe kumwera cikho ca Ambuye, ndi cikho ca ziwanda; simungathe kulandirako ku gome la Ambuye, ndi ku gome la ziwanda. (1 Akorinto 10:21)

SATANA ALI NDI ATUMIKI:

Mulungu anaitana okhulupirira ena kuti akatumikire ngati abusa ndi atumiki ku mpingo wake polalikira Uthenga wabwino (1Akorinto 12:28). Satana naye alinawo atumiki:

Ndipo kulibe kudabwa; pakuti Satana yemwe adzionetsa ngati mngelo wa kuunika. Cifukwa cace sikuli kanthu kwakukuru ngatinso atumiki ace adzionetsa monga atumiki a cilungamo; amene cimariziro cao cidzakhala monga nchito zao. (2 Akorinto 11:14-15)

Atumiki a satana amafalitsa uthenga wake omwe ndi wosiyana ndi Uthenga wabwino wa Ambuye Yesu Kristu:

umene suli wina; koma pali ena akubvuta inu, nafuna kuipisa Uthenga Wabwino wa Kristu. Koma ngakhale ife, kapena mngelo wocokera Kumwamba, ngati akakulalikiireni uthenga wabwino wosati umene tidakulalikirani ife, akhale wotembereredwa. (Agalatiya 1:7-8)

Chifukwa chakuti uthenga ukuperekedwa mwa mphamvu ndi mozizwitsa izi sizimatathauza kuti ndi Uthenga wabwino umene uli wowona.

SATANA ALI NDI MPANDO WACHIFUMU:

Mulungu ali ndi mpando wachifumu kumwamba. Satana naye alinso ndi mpando wachifumu, ngakhale sitinawuzidwe bwino bwino komwe uli:

Cibvumbulutso 2:2 Ndidziwa nchito zako, ndi cilemetso cako ndi cipiriro cako, ndi kuti sukhoza kulola oipa, ndipo unayesa iwo amene adzicha okha atumwi, osakhala atumwi, nuwapeza onama; (Chibvumbulutso 13:2)

SATANA ALI NDI OMULAMBIRA:

Pali anthu ambiri amene amalambira Mulungu wowona. Naye satana alinawo omulambira:

Ndipo analambira cinjoka, cifukwa cinacipatsa ulamuliro ciromboco; ndipo analambira cirombo ndi kunena, Manana ndi cirombo ndani? Ndipo akhoza ndani kugwira nkondo naco? (Chibvumbulutso 13:4)

Ena olambira satana amanamizira kumakhala ngati ndiwotsatira Yesu:

ndipo munda ndiwo dziko lapansi; ndi mbeu yabwino ndiyo ana a Ufumuwo; ndi namsongole ndiye ana a woipayo; ndipo mdani amene anamfesa uwu ndiye mdierekezi: ndi kututa ndico cimariziro ca nthawi ya pansu pano; ndi otutawo ndiwo angelo. (Mateyu 13:38-39)

Satana amasakaniza “mbeu” zoipa mu “mbeu” zabwino (okhulupirira eni eni).

SATANA ALI NDI ANENERI:

Mulungu anasakha aneneri mu mpingo, amuna amene anadzodzedwa mwapaderadera kuti azibweretsa uthenga ochokera kwa Iye kupita ku mpingo (1 Akorinto 12:28). Naye satana ali nawo aneneri ake:

Ndipo aneneri onama ambiri adzauka, nadzasokeretsaanthuambiri. (Mateyu 24:11)

SATANA ALI NDI APHUNZITSI:

Mulungu anadzodza anthu ena ngati aphunzitsi kuti akafotokozere Mau ake kwa ena (1Akorinto 12:28). Koma aphunzitsi onse siochoka kwa Mulungu. Satana ali ndi aphunzitsi onyenga amene amafalitsa chiphunzitso choipa.

Koma padakhalanso pakati pa anthuwo aneneri onama, monganso padzakhala aphunzitsi onama pakati pa inu, amene adzalowa nayo m'tseri mipatuko yotayikitsa, nadzakana Ambuye amene adawagula, nadzadzitengera iwo okha citayiko cakudza msanga. Ndipo ambiri adzatsata zonyansa zao; cifukwa ca iwo njira ya coonadi idzanenedwa zamwano. (2 Petro 2:1-3)

Aphunzitsi a satana amabweretsa “mphekesera zakuchiwonongeko,” chiphunzitso chomwe ndi ndi chabodza chomwe chimabweretsa magawanikano. Amayakhula mabodza ndipo ndi akatswiri odziwa kusakaniza choonadi chi zolakwika munjira yakuti zolakwaika zawaonzo zimalandiridwa.

SATANA ALI NDI ATUMWI:

Mtumwi ndi munthu amene amafalitsa Uthenga Wabwino ndikukhazikitsa mipingo (1Akorinto 12:28). Satana naye ali nawonso atumwi amene akugwira ntchito yake mu dziko lapansi. Amanyenga anthu pokoperera atumwi enieni:

Pakuti otere ali atumwi onyenga, ocita ocenjerera, odzionetsa ngati atumwi a Kristu, (2Akorinto 11:13)

Atumwi a Satana amakhala atsogoleri a zipembedzo zonama ndipo amalowerera mipingo ndipo amakhalanso atsogoleri a mpingo.

SATANA AMADZUTSA AKRISTU ONAMA:

Satana wakopera ngakhale Ambuye Yesu podzutsa a Kristu onama. Yesu anachenjeza:

Ndipo Yesu anayankha nati kwa iwo, Yang'anirani, asasokeretse inu munthu. Pakuti ambiri adzafika m'dzina lan ga, nadzanena, Ine ndine Kristu, nadzasokeretsa anthu ambiri. (Mateyu 24:4-5)

A kristu onyengawa amagwiritsa ntchito dzina la Yesu. Amachita zozizwa ndi zizindikiro zambiri. Koma ndi okopera mphamvu ya Mulungu.

SATANA ALI NDINJIRA ZOLUMIKIZIRANA:

Baibulo linalemba mmene Mulungu amakamuyakhulira munthu munthawi yakale. Mulungu akupitirizabe kuyakhula kwa munthu mpakana lero. Satana naye amayakhulanso kwa munthu. Mau ake oyamba amene anayakhula kwa munthu anapangitsa munthu kuti achimwe (Genesis chaputala 3).

Okhulupirira amapephera kwa Mulungu malingana ndi zosowa zawo. Mulungu amayakha pephero la olungama (Yakobo 5:16). Otsatira satana amapephera kwa iye ndipo amalumikizana ndi mizimu yoipa. Nthawi zina satana amayakha ndi zinthu zoposa chilengedwe monga ngati mau, kuyenda kwa zinthu, mphokoso, ndizina zotero. Satana ali ndi mphamvu zenizeni ndipo atha kuwonetsera mphamvu zimenezi pochita zinthu zowoneka ndi maso.

Mulungu amayakhulana ndi munthu kudzera mmau Ake olembedwa, Baibulo. Chonchoso uthenga wa satana nawo umafalitsidwa kupyolera mu mau olemba ndi zolembedwa zoipa, mabuku, zithuzi, makanema ndi nyimbo. Uthenga wochokera kwa Mulungu kudzera mmau Ake olembedwa ndi kuyakhulidwa umapereka chitsogonzo kwa munthu muzochitika za moyo.

Satana ali ndi njira yonama yomwe imatsogozwa ndipo imakwaniritsidwa potsata njira zotsatirazi:

Potsata nyenyezi: Amagwiritsa ntchito nyenyezi polosera zochitika ndi kupereka chitsogozo.

Pakuweranga masamba a tea, zinthuzi, mizere mmutu, mizere ya mmanja ndi mipira yonyezimira:

Uthega wamasamba a tea, mizere ya mmanja mwa munthu, mipira yonyezimira, ndi zithuzi zimanenedwa kuti zimapereka chitsogozo.

Ufiti: pogwiritsa ntchito zamatsenga, zanyanga, zamaula, zoombeza, zaufiti, njira zofuna kupeza mwayi, masophenya, zonzambula, ndi zina zofanana nazo zomwe siziri malemba kuti alandire chidziwitso.

SATANA ALI NDI MPHAMVU ZOPOSERA CHILENGEDWE:

Yesu analonjeza mphamvu zopambana kwa omutsatira pamene adzadzadzidwa ndi Mzimu Woyera (Machitidwe 1:8). Satana nayeso amapereka mphamvu zoposa ulamuliro

(Chibvumbulutso 13:2). Ziwanda zake zimalenga mphamvu. Satana amapereka mphamvu ndi ulamuliro omwe (Chibvumbulutso 13:2), monga momwe Yesu amachitira. Satana angathe kupanga zizindikiro ndi zozizwa za mphamvu:

pakuti ali mizimu ya ziwanda zakucita zizindikilo; zimene zituruka kumka kwa mafumu a dziko lonse, kuwasonkhanitsira ku nkondo ya tsiku lalikuru la Mulungu, Wamphamvuyonse. (Chibvumbulutso 16:14)

Yesu anati:

Ambiri adzati kwa Ine tsiku lomwelo, Ambuye, Ambuye, kodi sitinanenera mau m'dzina lanu, ndi m'dzina lanunso kuturutsa mizimu yoipa, ndi kucita m'dzina lanunso zamphamvu zambiri? Ndipo pamenepo ndidzafukulira iwo, Sindinakudziwani inu nthawi zonse; cokani kwa Ine, inu akucita kusayeruzika. (Mateyu 7:22-23)

Zindikirani kuti Yesu anati “Sindikudziwani inu.” Anthu amenewa amawonetsa mphamvu zozizwitsa koma sanali a Mulungu. Anali onyenga okopera.

MPHAMVU ZOPAMBANA

Satana ndiwotsutsa wokopera weniweni. Ali ndi dongosolo la mphamvu. Omutsatira ake amatha kuchita zinthu zamphamvu. Yesu anachenjeza za mphamvu Yake:

Koma ndidzakulangizani amene muzimuopa; taopani iye amene atatha kupha ali ndi mphamvu yakutaya kugehena, inde, ndinena ndinu opani ameneyo. (Luka 12:5)

Koma Mulungu ali ndi mphamvu zopambana. Yesu anati:

Inu ndinu ocokera mwa Mulungu, tiana, ndipo munailaka; pakuti iye wakukhah mwa inu aposa iye wakukhala m'dzi ko lapansi. Iwo ndiwo ocoken m'dziko lapansi; (1 Yohane 4:4)

Muphonzira mu chaputala chotsatirachi mmene Yesu anabwerera ndi mphamvu zopambana ndi ulamuliro kuzawononga ntchito zoipa za satana. Muphonzira machaputala otsatira mmene Yesu anaperekeram mphamvu zake kwa okhulupirira kuposera mphamvu za mdani.

KUKUMANA NDI CHITSUTSO CHOKOPERA

Izi ndi zina mwa ndondomeko zomwe Baibulo limakamba kuti tigwiritse ntchito pofuna kukumana ndi mphamvu zotsutsa zokopera.

KUGWIRITSA NTCHITO CHIDZIWITSO:

Pali mphatso yapaderadera ya Mzimu Woyera imene imatchulidwa kuti kuzindikira mizimu. Ndikuthekera komwe kumaperekedwa ndi Mulungu kuti mwachangu changu uzindikire mzimu wa munthu wina ndi kudziwa ngati uli wabwino kapena woyipa. Ngati muli ndi mphatso ya uzimu, igwiritseni ntchito pozindikira ngati mizimu ya anthu ili yochokera kwa Mulungu kapena kwa Satana.

Ngati mulibe mphatso imeneyi, Mulungu waperekaso njira ina yozindikirira. 2 Petro 2 ndi buku la Yuda limakamba machitachita a anthu amizimu yoyipa zomwe zingakuthandizeni kuti muwazindikire iwo. Posatengera kuti munthu ndi wauzimu kapena ndi wamphamvu zotani, mukuyenera kuwayeza ndi Mau a Mulungu.

KUSATHULA MPHAMVU NDI CHIPATSO CHAKE:

Chifukwa chakuti satana amakopera mphamvu ya Mulungu kupyolera mu mphamvu yowonetsera zozizwa, zizindikiro, ndi zodabwitsa, Mulungu wapereka njira yosathulira mautumiki. Yesu anafananitsa anthu ndi mtengo wa zipatso:

Sungathe mtengo wabwino kupatsa zipatso zoipa, kapena mtengo wamphuci kupatsa zipatso zokoma. Mtengo uli wonse wosapatsa cipatso cokoma, audula, nautaya kumoto. Inde comweco pa zipatso zao mudzawazindikira iwo. (Mateyu 7:18, 20)

Satana amatha kukopera mphatso za uzimu ndi mphamvu ya Mulungu, koma sangakopere moyo wa chiyero ndi kuwonetsera chipatso cha Mzimu Woyera:

Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, icikhulupirtro, cifatso, ciletso; pokana zimenezi palibe lamulo. (Agalatiya 5:22-23)

Sathulani mautumiki ndi chipatso cha Mzimu mmalo mwakuwonetsera mphamvu.

KUPHUNZIRA MAU A MULUNGU:

Pofuna kuzindikira chiphunzitso chonyenga chomwe aphuzitsi, atumwi, aneneri ndi mautiki asatana, mukuyenera kuzindikira chomwe chanenedwa mu mau a Mulungu. Paulo anamuza Timoteo:

Ucite cangu kudzionetsera kwa Mulungu wobvomerezeka, wanchito wopanda cifukwa ca kucita manyazi, wolunjika nao bwino mau a coonadi. (2 Timoteo 2:15)

Ngakhale Paulo anali mtsogoleri wopambana wa Uzimu mu mpingo woyamba, okhulupirira ku mpingo waku Bereya amkakasathulaso china chirichonse chomwe anakamba kuchokera mmau a Mulungu olembedwa:

Amenewa anali mfulu koposa a m'Tesalonika, popeza analandira mau ndi kufunitsa kwa mtima wonse, nasanthula m'malembo masiku onse, ngati zinthu zinali zotero. (Machitidwe 17:11)

Popewa kunyengedwa ndi mphamvu za satana, yesani china chirichonse chomwe champhunzitsidwa ndi Mau a Mulungu. Sathulani miyoyo ya onse amene akuphunzitsa ziphunzitso zamphamvu komaso iwo amene akupanga zizindikiro ndi zozizwa.

Osamangolandira chiphunzitso chirichonse, bvumbulutso, kapenaso chozizwa chomwe sichikugwirizana ndi Mau a Mulungu. Mphamvu ya satana imakopa anthu okhulupirira pakudzera kuzomwe zimatchulidwa kuti “Bvumbulutso lapaderadera la chowona chatsopano.” Anthu amanena kuti ali ndi maloto apaderadera, omwe amawonetseredwa ndi angelo, masomphenya, mau, komaso ndi zina zapaderadera zomwe zimabwera mwa mphamvu.

Koma Paulo anachenjeza:

umene suli wina; koma pali ena akubvuta inu, nafuna kuipsa Uthenga Wabwino wa Kristu. Koma ngakhale ife, kapena mngelo wocokera Kumwamba, ngati akakulalikireni uthenga wabwino wosati umene tidakulalikirani ife, akhale wotembereredwa. (Agalatiya 1:7-8)

Musamavomere china chirichonse chotchulidwa kuti uneneri omwe sukugwirizana ndi muyeso wachikhulupiriro (Aroma 12:6) ndipo chomwe sichingachitike (Deuteronomo 18:22).

Musamavomere bvumbulutso lirironse lomwe lingakupititseni kutali ndi Mulungu ndi kuchowonadi cha Mau Ake (Deuteronomo 13:1-5):

Munthu wosocera pa njira ya nzeru Adzakhala m'msonkhano wa akufa. (Miyambo 21:16)

MUZIPEWA MACHENJERERO ALIWONSE ASATANA:

Mulungu anachenjeza Israeli kuti apewe mtundu wina uliwonse wamachenjerero a satana:

mupitikitse onse okhala m'dzikopamaso panu, ndi kuononga mafano ao onse a miyala, ndi kuononga mafano ao onse oyenga, ndi kupasula misanje yao yonse; (Numeli 33:52)

Werengani malangizo owonjezera amene Mulungu anapereka mu Deutolonomo 18:9-14. Israeli samayenera kukhala paubale ndi ntchito ya satana mwanjira ina iliyonse. Muwononge china chirichonse chomwe chimakhudzana ndi ufiti kapena ndi ntchito ina iriyonse ya ziwanda. Izi ndikuphatikizapo, mafano, makhwala opatsa mwayi, zithumwa, masewero, zamdziko, ndi zinthu zina zofanana nazo. Onongani zolembedwa zoipa ndi nyimbo zomwe sizikweza Mulungu. Izi ndi zomwe anthu anachita mu Chipangano Chatsopano pamene anakhala okhulupirira:

Ndipo ambiri a iwo akucita zamatsenga anasonkhanitsa mabuku ao, nawatentha pamaso pa onse; ndipo anawerenga mtengo wace, napeza ndalama zasiliva zikwi makumi asanu. Machitidwe 19:19)

Musamathe nthawi yanu kukhala pamalo pomwe pali machitachita oipa. Baibulo limanena kuti Mulungu amaziwonetsera Yekha pamalo omwe ali opatulika monga makachisi m'Chipango Chakale komaso pachipinda chapamwamba m'nyumba muja patsiku la Pentekosti. Nde zoona zake ndi zakuti nayo mphamvu ya satana itha kuwonekera pamaloso opatulika omwe operekedwa ku zoipa. Malo awa akhoza kukha komwe kumawonetsedwa kanema, malo omwerako mowa komwe khalidwe lonyasa limachitika, malo amene kumachitika juga, satana amapembedzedwa pamalo pali ponse pamene pakuchitika zauchimo. Muzipewa kupeza mmalo amenewo, chifukwa mphamvu ya satana mmalo amenewo imakhala yolimba kwambiri. Simungapephere, "Musatitengere kokandiyesa," kaneko mukapezekaso mmalo amenewo.

Koma nditi kuti zimene amitundu apereka nsembe azipereka kwa ziwanda; ndipo sindifuna kuti inu muyanjane ndi ziwanda. (1 Akorinto 10:20)

Musamayanjane nawo atsogoleri, aneneri, atumiki ngakhaleso atumwi onama.

Pewani mawonekedwe onse achoipa. (1 Atesolanika 5:22)

ZINDIKIRANI KUTI MPHAMVU YAMULUNGU KUTI NDIYOPAMBANA KWAMBIRI KUPOSA YA SATANA:

Dongosolo la Mulungu, mpingo wowona, ndi zamphamvu kwambiri kuposa satana.

ndipo anakonza zonse pansi pa mapazi ace, nampatsa iye 4 akhale mutu pamtu pa zonse, 5 kwa Eklesia amene ali thupi lace, 6 mdzazidwe wa iye amene adzazazonse m'zonse. (Aefeso 1:22-23)

kuti mu Eklesia azindikiritse tsopano kwa akulu ndi maulamuliro m'zakumwamba nzeru ya mitundu mitundu ya Mulungu, (Aefeso 3:10)

Yesu ndi mutu wa mpingo. Okhulupirira ndi thupi. Ngati zinthu zonse (kuphatikizapo satana ndi mndandanda wachipembedzo chake) ziri pasi pa mapazi a Yesu, ndekuti ziriso pansi pa mapazi athu chifukwa ife ndi thupi. “Pansi pamapazi” zikutathauza ali pansi pa mpamvu ndi ulamuliro omwe Mulungu watipatsa ife. Yesu anati tiri ndi mphamvu pamwamba “mphamvu zonse za mdani” (Luka 10:19). Izi zikuphatikizapo kuipa kwa uzimu mmiyamba. Satana ndi amthenga ake amalimbana ndi mphamvu ya Mulungu, koma sikuti ndichiopsyezo kwa Iye kapena anthu Ake. Zowona zake ndi zakuti mpingo ndi chiwonetsero cha mphamvu ya Mulungu kwa maukulu ndi mphamvu ya oipa!

PHUNZIRANI NDONDOMEKO ZA ZAMPHAMVU ZOMWE BAIBULO LIMAKAMBA:

Muphunzira ndondomeko za Baibulo mu phunziro lino. Ngati mungamvetsetse ndondomeko ya mphamvu ya Mulungu, simuzanyengedwa ndi ntchito zokopera za satana.

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yoloweza yapamtima.

2. Kodi kunena kuti “kuiipa kwa uzimi miyamba” zutathauza chani?

3. Lembani mwachidule zonse zomwe mukumbukira zokhudzana ndi ndikukopera mphamvu ya Mulungu ndi satana kudzala kukuipa kwa mizimu mmiyamba.

4. Lembani ndondomeko zisanu ndi zitatatu za m’Baibulo zomwe zaperekedwa mu chaputala chino zomwe zingakuthandizeni kuti mupambane ku mphamvu ya wotsutsa wokopera.

(Mayankho amayesowa aperekedwa kumapeto kwa buku lino.)

ZOWONJERA POPHUNZIRA

1. Phunzirani 2 petro chaputala 2 ndi buku la Yuda. Machaputala awa akuthandizani kuti muzindikire otsatira satana mumpingo.
2. Pezani phunziro la The Harvestime International Institute “Ndondomeko ya za uzimu”: Buku la Nkhondo ya Uzimu”. Likuthandizani kuti muphunzire zambiri zokhudzana ndi kulimbana ndi chinyengo komaso limapereka ndondomeko zomwe zimathandiza kuti mupambane.
3. Monga ngati otsanzira mphamvu ya Mulungu, satana akufunafuna kuti anyenge ambiri lero mdziko. “Kunyenga” ndiko kuti kupotoza kapena kumupanga wina kuti akhulupirire chinthu chomwe sichiri chowona.
 - Satana samangonamiza anthu okha koma amanamizanso ngakhale maiko: Chibvumbulutso 20:8-9
 - Satana amagwira ntchito ndi “m’chinyengo chonse cha chosalungama”: 2 Atesalonika 2:10
 - Tikuchenjezedwa kuti chinyengo chidzakula. 2 timoteo 3:13
 - Chifukwa chakuti chinyengo chidzakula, tikuyenera kuti tikhale tcheru ndi zochitika zomwe zimawonetsera kubwera kwa Kristu. Mateyu 24; Marko 13; 2 Atesalonika 2:3
 - Tachenjezedwa kuti tikhale tcheru ndi amene satana amawagwiritsa ntchito kuti anyenge anthu: 2 Akorinto 11:13; Tito 1:10; 2 Petro 2:13; 2 Yohane 7
 - Mtima wa munthu ndi onyenga: Yeremiya 17:9
 - Munthu wina aliyense osapulumsidwa ndionyengedwa: 2 Akorinto 4:4; Ahebri 3:13
 - Musamavomere chinyengo “mau okoma ndi osyasyalika” amene samavomerezana ndi Mau a Mulungu: Aroma 16:18; 2 Akorinto 4:2

Mwanyengedwa ngati...

- Mukumvetsera nzeru zopanda pake: Akolose 2:8

- Mukukhulupirira chuma ndi kulola zilakolako za nthupi: Mateyu 13:22; Marko 4:19; Aefeso 4:22
- Ndinu ongomva chabe koma osachita Mau a Mulungu: Yakobo 1:22
- Mukuti mulibe ntchimo lirilonse: 1 Yohane 1:8
- Mukumvera anthu oipa: 2 3:13
- Pamene mukuganiza kuti ndi ofunika kwambiri pamene ndinu osafunika: Agalatiya 6:3
- Mukuganiza kuti simuzakolola zomwe mwafesa: Agalatiya 6:7
- Mukuganiza kuti osalungama azalowa mu ufumu wa Mulungu: 1 Akorinto 6:9
- Mukuganiza kuti ndinu ozindikira chifukwa muli ndi nzeru zadziko lino: 1 Akorinto 3:18
- Muziyesa kuti ndinu auzimu koma kusamanga lilime kumaulula cheni cheni chomwe muli: Yakobo 3:26
- Simukhulupirira kuti Yesu Christu anabwera ku nthupi: 2 Yohane 7
- Mukuganiza kuti kukhudzana ndi tchimo sikungapereke mvuto kwa inu: 1 Akorinto 15:33

CHAPUTALA 4

“PALIBE MUNTHU AMENE ANAYAKHULA NGATI IYE”

ZOLINGA:

Pamapeto pamaphunziro awa mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osawonera.
- Kufotokoza gwero a mphamvu za Yesu.
- Kulemba mwachidule zomwe Baibulo limaphunzitsa zokhudzana mphamvu ndi ulamuliro wa Yesu.

VESI YOTSOGOLERA:

Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine kumwamba ndi dziko lapansi.(Mateyu 28:18).

MAU OYAMBA

Utatu wa Mulungu umapangidwa ndi Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Gwero la mphamvu ndi Mulungu Atate. Mulungu anapereka mphamvu kwa Mwana Wake, Yesu Kristu. Kenako Mzimu Woyera anawadzadza okhulupirira ndi mphamvu zomwe analandira kuchokera kwa Mwana.

Mu chaputala ichi muphunzira za mphamvu ndi ulamuliro wa Yesu. Zinali zapamwamba kuti atsogoleri achipembedo munthawi Yake anayankhula kuti, ”Palibe munthu aliyense analakhula ngati Iye” (Yohane 7:46)

KUBADWA MU MPHAMVU

Yesu anabadwa mumphamvu ya Mzimu Woyera:

Ndipo mngelo anayankha, nati kwa iye, Mzimu Woyera adzafika pa iwe, ndi mphamvu ya Wamkulukulu idzakuphimba iwe: cifukwa cacenso Coyeraco cikadzabadwa, cidzachedwa Mwana wa Mulungu. (Luka 1:35)

Yesu anali anawonetseredwe ndi amphamvu ya Mulungu yowoneka:

koma kwa iwo oitanidwa, ndiwo Ayuda ndi Ahelene, Kristu 1 mphamvu ya Mulungu, ndi 2 nzeru ya Mulungu. (1 Akorinto 1: 24)

KUBATIZIDWA MU MPHAMVU

Yohane anazindikira mphamvu za Yesu. Anati:

Ndipo analalikira, kuti, Wondipambana ine mphamvu akudza pambuyo panga, sindiyenera kuwerama kumasula lamba la nsapato zace ine. Ndakubatzani inu ndi madzi; koma Iye adzakubatzani ndi Mzimu Woyera. (Marko 1:7-8)

Pamene Yesu amkabatizidwa ndi Yohane mu mtsinje wa Yolodano, Mzimu Woyera anatsikira pa Iye monga nkunda:

Ndipo sindinamdziwa iye; koma kuti aonetsedwe kwa Israyeli, cifukwa ca ici ndinadzaine kudzabatiza ndi madzi. (Yohahe 1:31)

Mulungu anamuza Yohane...

Ndipo sindinamdziwa iye, koma wonditumayo kudzabatiza ndi madzi, Iyeyu ananena ndi ine, Amene udzaona Mzimu atsikira, nakhala pa iye, 9 yemweyu ndiye wakubatzani ndi Mzimu Woyera. (Yohane 1:33)

Ichi chinali chitsimikizo pamena Mzimu Woyera anakhala pa Yesu mumawonekedwe a nkunda. Yesu sikuti anangodzadzidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera, koma anabatizidwaso ndi Mphamvu.

KUTSIMIKIZIRIDWA KWA MPHAMVU

Atangotha kubatizibwa, Yesu anapita kuchipululu ku kayesedwa ndi satana:

Ndipo Yesu, wodzala ndi Mzimu Woyera, anabwera ku Yordano, natsogozedwa ndi Mzimu kunka kucipululu kukayesedwa ndi mdierkezi masiku makumi anai. (Luka 4:1)

Mukhoza kuwerenga za mmene anayeseredwera pa Luka 4:1-13.

Mphamvu zimatsimikiziridwa pakuyesedwa. Yesero lina lirironse la satana linatsutsana ndi mphamvu ndi ulamuliro wa Yesu. Yesu anakwanitsa kupambana yesero linalirilonse ndipo...

Yesu anabwera ndi mphamvu ya Mzimu ku Galileya; ndipo mbiri yace ya iye inabuka ku dziko lonse loyandikira. (Luka 4:14)

KOCHOKERA MPHAMVU ZAKE

Mulungu Atate kunali kochokera mphamvu ndi ulamuliro wa Yesu. Yesu anati:

Mzimu wa Ambuye uli paine, Cifukwa cace iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino: Anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru ophwanyika, Kulalikira caka cosankhika ca Ambuye. (Luka 4:18-19)

Yesu sanagwiritse ntchito mphamvu pa Yekha popanda Mulungu Atate. Mu utumiki Wake pano padziko lapansi, Yesu amatamanda Mulungu ngati kochokera mphamvu Zake.

Yesu anayankha iwo, ndakuonetsani inu nchito zabwino zambiri za kwa Atate; cifukwa ca nchito yiti ya izo mundiponya miyala? (Yohane 10:32)

MPHAMVU YOPANDA MALIRE

Mphamvu za Yesu zinalibe malire. Anapatsidwa ulamuliro onse Kumwamba ndi dziko lapansi:

Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi. (Mateyu 28:18)

Yesu anali ndi mphamvu:

pamwamba pa ukulu wonse, ndi ulamuliro ndi mphamvu, ndi ufumu, ndi dzina liri lonse lochedwa, si m'nyengo yinoya pansu pano yokha, komanso mwaiyo ikudza; ndipo 3 anakonza zonse pansu pa mapazi ace, nampatsa iye 4 akhale mutu pamtu pa zonse, (Aefeso 1:21-22)

Yesu ndi mutu wa mphamvu zonse:

ndipo muli odzazidwa mwa iye, ndiye mutu wa ukulu wonse ndi ulamuliro; (Akolose 2:10)

Yesu anali ndi mphamvu zopanda malire. Anapatsidwa:

MPHAMVU ZOPHUNZITSA NDI ULAMULIRO:

Alembi ulamuliro wawo umkakhazika pa malemba a M'chipangano Chakale. Ulamuliro wa Yesu umakakhazikika pa Mulungu Yekha.

Ndipo anazizwa ndi ciphunzitso cace; pakuti anaphunzitsa monga mwini mphamvu, si monga alembi. (Marko 1:22)

cifukwa mau ace anali ndi ulamuliro. (Luka 4:32)

MPHAMVU PA TCHIMO:

Yesu anali ndi mphamvu zokhululukira tchimo:

Koma kuti mudziwe kuti ali nazo mphamvu Mwana wa munthu pansi pano za kukhululukira macimo (pomwepo ananena kwa wodwalayo), Tanyamuka, nutenge chika lako, numuke kunyumba kwako. (Mateyo 9:6)

MPHAMVU PAMATENDA:

Ndipo pakudza madzulo, anabwera nao kwa Iye anthu ambiri ogwidwa ndi mizimu yoipa; ndipo Iye anaturutsa mizimuyo ndi mau, naciritsa akudwala onse; (Mateyu 8:16)

MPHAMVU PA CHILENGEDWE:

Ndipo anauka, nadzudzula mphepo, nati kwa nyanja, kuti, Tonthola, khala bata. Ndipo mphepo inaleka, ndipokunagwa bata lalikuru. (Marko 4:39)

MPHAMVU PA NTHUPI LIRI LONSE:

monga mwampatsa iye ulamuliro pa thupi liri lonse, kuti onse amene mwampatsa iye, awapatse iwo moyo wosatha. (Yohane 17:2)

MPHAMVU PA ADANI AKE:

Cifukwa cace Pilato ananena kwa iye, Simulankhula ndi ine kodi? simudziwa kodi kuti ulamuliro ndiri nao wakukumasulani, ndipo ndiri nao ulamuliro wakukupacikani? Yesu anamyankha iye, Simukadakhala nao ulamuliro uli wonse pa Ine, ngati sukadapatsidwa kwa inu kucokera Kumwamba; cifukwa ca ici iye wondipereka Ine kwa inu ali nalo cimo loposa. (Yohane 19:10-11)

MPHAMVU PA IMFA:

Yesu anati:

Yesu anati kwa iye, Ine ndine kuuka ndi moyo; wokhulupirira Ine, angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo; (Yohane 11:25)

Kupholera mu imfa ndi chiukitso Chake...

atabvula maukulu ndi maulamuliro, anawaonetsera poyera, nawagonjetsera nako. (Akolose 2:15)

MPHAMVU PA MOYO WAKE OMWE:

Palibe wina andicotsera uwu, koma ndiutaya Ine ndekha. Ndiri nayo mphamvu yakuutaya, ndi mphamvu ndiri nayo yakuutenganso; lamulo ili ndinalandira kwa. Atate wanga. (Yohane 10:18)

MPHAMVU YOPEREKA CHIWERUZO:

Mulungu wapereka mphamvu kwa Yesu yopereka chiweruzo:

ndipo anampatsa iye mphamvu ya kucita mlandu, pakuti ali Mwana wa munthu. Yohane 5:27)

MPHAMVU PA ZIWANDA:

Ndipo anthu onse anadabwa, nalankhulana wina ndi mnzace, nanena, Mau amenewa ali otani? cifukwa ndi ulamuliro ndi mphamvu angolamulira mizimu yonyansa, ndipo ingoturuka. (Luka 4:36)

Ndipo anazizwa onse, kotero kuti anafunsana mwa iwo okha, kuti, Ici nciani? ciphunzitsa catsopano! ndi mphamvu alamula ingakhale mizimu yonyansa, ndipo imvera Iye. (Marko 1:27)

za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Machitidwe 10:38)

MPHAMVU PA NTCHITO ZONSE ZA MDANI:

Cholinga chimene Yesu anabwerera pa dziko lapansi chinali chozaononga ntchito zonse za mdierekezi.

iye wocita cimo ali wocokera mwa mdierekezi, cifukwa mdierekezi amacimwa kuyambira paciyambi. Kukacita ici Mwana wa Mulungu adaonekera, ndiko kuti akaononge nchito za mdierekezi, (1 Yohane 3:8)

MPHAMVU YAPANOPA

Potsatira imfa ndi chiukutso Chake, Yesu anabwerera kumwamba. Kumeneko akupitiriza kutumikira mu mphamvu ndi ulamuliro ku dzanja la manja la Mulungu:

kuyambira tsopano Mwana wa munthu adzakhala pa dzanja lamanja la mphamvu ya Mulungu. (Luka 22:69)

Taonani, 26 ndipenya m'Mwamba motseguka, ndi Mwana wa munthu alikuimirira pa dzanja lamanja la Mulungu. (Machitidwe 7:56)

Yesu akupitirizabe kutumikira kupyolera mu mphamvu zomwe zapatsidwa kwa okhulupirira. Yesu asanabwerere kumwamba, anapereka mphamvu ndi ulamuliro kwa omutsatira Ake. Amayenera kuchita ntchito imene Iye amkachita, ngakhale kuposera apo (Yohane 14:12). Muphunzira za kuperekedwa kwa mphamvu mu chaputala chotsatira.

MPHAMVU YOMTSOGOLO

Tsiku lina, Yesu adzabweraso pa dziko lapansi ndi mphamvu yayikulu ndi ulemerero:

ndipo pomwepo padzaoneka m'thambo cizindikiro ca Mwana wa munthu; ndipo mitundu yonse ya pa dziko lapansi idzadziguwala pacifuwa, nidzapenya Mwana wa munthu alinkudza pa mitambo ya kumwamba, ndi mphamvu ndi ulemerero waukuru. (Mateyu 24:30)

Panthawi imeneyo mphamvu zonse zakumwamba ndi dziko lapansi zizaperekedwa kwa Yesu:

Pomwepo pali cimariziro, pamene adzapereka ufumu kwa Mulungu, ndiye Atate, atatha kuthera ciweruzo conse, ndi ulamuliro wonse, ndi mphamvu yomwe. (1 Akorinto 15:24)

Dziko lonse lizamvomereza mphamvu ya Mulungu Atate ndi Mwana, Yesu kristu:

akunena ndi mau akulu, Ayenera Mwanawankhosa, wophedwayo, kulandira cilimbiko, ndi cuma, ndi nzeru, ndi mphamvu, ndi ulemu, ndi ulemerero, ndi ciyamiko. (Chibvumbulutso 5:12-)

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Kodi zotchinga za mphamvu ya Yesu zinali ziti?

3. Kodi anali ndani amene amamphatsa Yesu mphamvu ndi ulamuliro?

4. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira muchaputala ichi zokhudzana ndi mphamvu ndi ulamuliro wa Yesu.

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa buku lino)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Pitirizani kuphunzirabe zokhudzana ndi mphamvu ndi ulamuliro wa Yesu pophunzira za moyo ndi utimiki Wake mu buku la Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane.

Muzisunga mbiri ya nthawi zomwe Yesu amkapereka mphamvu zake kwa Mulungu Atate: kakwana kangati?

Muzisunga mbiri ya momwe amkaonetsera mphamvu Yake mukuphunzitsa, kuchiritsa, kutulutsa ziwanda, zozizwa, kulamula chilengedwe, ndi zina zotero. Gwiritsani tchito tchati:

Malemba

Momwe mphamvu inawonetsedwera

Zotsatira

CHAPUTALA 5

MPHAMVU YOPATSIDWA

ZOLINGA:

Pamapeto pa phunziro iri mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osawonera.
- Kunena gwero la komwe timalandira ulamuliro wa uzimu.
- Kufotokoza ngwirizinao pakati pa udindo ndi mphamvu.
- Kufotokoza udindo omwe Yesu anapereka kwa Ophunzira Ake.
- Kupereka tanthauzo la mau awiri a chigiriki.

VESI YOTSOGOLERA:

Taonani, ndakupatsani ulamuliro wakuponda pa njoka nsi zinkhanira, ndi pa mphamvu iri yonse ya mdaniyo; ndipo kulibe kanthu kadzakuipsani konse. (Luka 10:19).

MAU OYAMBA

Mulungu nde chiyambi cha mphamvu. Anapereka “mphamvu zonse” kwa Mwana Wake, Yesu Kristu. Keneko Yesu anapereka mphamvu za uzimu kwa Omutsatira Ake. Mphamvu imeneyi inawapangitsa iwo kudzala ndi udindo waukulu omwe unaperekedwa kwa iwo.

UDINDO NDI ULAMULIRO

Pamene Yesu anamaliza utumiki Wake padziko pano ndikubwerera kumwamba, anawasiya omutsatira ndi udindo waukulu. Anawalamula kuti:

Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano. (Mateyu 28:19-20)

Udindo omwe Yesu anapereka kwa otsatira Ake unali oti akafikire dziko lonse lapansi ndi Uthenga Wabwino wa ufumu wa Mulungu.

Pali kugwirizana kwakukulu pakati pa udindo ndi ulamuliro. Pamene wina akupatsidwa udindo wakuti achite china chake, akuyenera apatsidweso mphamvu yochita chimenecho. Ulamuliro umenewo ukuyenera kuperekedwa ndi munthu wina amene ali woposera wolandilayo..

Mwachitsanzo, wapolisi amapatsidwa udindo okhazikitsa bata mmudzi kapena mu mzinda. Amapatsidwaso ulamuliro ndi boma kuti akakwaniritse udindo omwe wapatsidwawo.. amapatsidwa ulamuliro wonyamula chida chomwe chimampatsa mphamvu yokwaniritisa ntchito yake. Wapolisi sakhala ndi ulamuliro payekha. Ulamuliro wake ndiwopatsidwa kwa iye ndi mabwana ake. Ndi munthu amene akugwira ntchito ndi mphamvu zomwe zapatsidwa kwa iye ndi omutsogolera amene ali pamwamba pake. Amakhala akuyimirira boma.

Yesu anawapatsa omutsatira Ake udindo okafikira dziko lonse lapansi ndi Uthenga Wabwino. Nde anawapatsanso ulamuliro okakwaniritisa ntchito. Simungampatse wina wake udindo popanda kumpatsanso ulamuliro oti akakwaniritse ntchito wapatsidwayo. Kodi ulamuliro umenewu unali uti? Unali wa uzimu. Yesu anati:

Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi. (Mateyu 28:18)

Kenako anazatinso:

(Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansu pano. (Mateyu 28:19-20)

ULAMULIRO OTUMA

Pamene Yesu anabwera pa dziko lapansi, anabwera ndi mphamvu ndi ulamuliro. Yesu anali ndi “mphamvu zonse” zomwe analandira kuchokera kwa Mulungu. Chifukwa cha ichi, Iye (Yesu) anali ndi ulamuliro opereka mphamvu ndi ulamuliro kwa otsatira Ake.

Ndipo pamene Iye anadziitanira ophunzira ace khumi ndi awiri, anapatsa iwo mphamvu pa mizimu yoipa, yakuiturutsa, ndi yakuciza nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 10:1)

Ndipo anadzodza nkhumu ndi awiri, kuti akhale ndi Iye, ndikuti awatume kukalalikira,

Ndipo anaika khumi ndi awiri, kuti akhale ndi Iye, ndi kuti akawatume kulalikira, ndi kuti akhale nao ulamuliro wakuturutsa ziwanda. (Marko 3:14-15)

Ndipo anadziitanira khumi ndi awiriwo, nayamba kuwatumiza Iwo awiri awiri; nawapatsa mphamvu pa mizimu yonyansa; (Marko 6:7)

Ndipo iye anaitana pamodzi khumi ndi awiriwo nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziwanda zonse, ndi zakuciritsa nthenda. (Luka 9:1)

Sanali madalitso akuthupi kapena zinthu zimene Yesu anapereka kwa ophunzira Ake.

Sanakhazikitse malo ku Yerusalemu komwe amachitirako ntchito yawo. Anadziwa kuti izi zisikakwaniritsa ntchito yomwe wawapatsa. Koma anawapatsanso mphamvu.

Mu chaputala 3 mwaphunzira zamphamvu ya satana. Mphamvu yomwe Yesu anapereka kwa otsatira Ake kuti ndiyoposa mphamvu ya mdaniyo.

Taonani, ndakupatsani ulamuliro wakuponda pa njoka ndi zinkhanira, ndi pa mphamvu iri yonse ya mdaniyo; ndipo kulibe kanthu kadzakuipsani konse. (Luka 10:19)

Satana sikuti amachita nanu mantha. Sikuti azakupatsa ulemu, koma amawopa ulamuliro omwe Mulungu anakupatsani. Ulamuliro umakhazikika kwambiri pa ubale. Mwachitsanzo, wa polisi ali ndi ulamuliro chifukwa cha ubale wake ndi boma. Ulamuliro wanu umakhazikika paubale ndi Ambuye Yesu Kristu. Kumbuyo kwanu kumaima Yesu ndi “mphamvu zonse.” Pamene mwazindikira chowonadi ichi, moyo wanu uzasithika. Yesu anawauza ophunzira:

Ndipo onani, 12 Ine nditumiza pa inu lonjezano la Atate wanga; koma khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yocokera Kumwamba. (Luka 24:49)

Buku la Machitidwe linalamba mmene lonjezano la mphamvu ya uzimu linakwanitsidwira miyoyo ya okhulupirira. Zozizwa, zizindikiro ndi zodabwitsa zomwe zalembedwa buku iri ndi zosangalatsa. Kuwonetseredwa kwina kulikonse kwa mphamvu ya Mulungu kumachitika ndi cholinga chokwaniritsa udindo wofikira dziko lonse ndi Uthenga Wabwino.

MAU AWIRI A MPHAMVU

Muchipangano Chatsopano, mau osiyana awiri a Chigriki amasuliridwa ndi liwu limodzi, mphamvu. Matanthuzo awiriwo anenedwa mu vesi iri:

Taonani, ndakupatsani ulamuliro (*exousia*) wakuponda pa njoka ndi zinkhanira, ndi pamphamvu (*dunamis*) yonse ya mdaniyo... (Luka 10:19)

Mau a Chigriki “*exousia*” amatanthauza kuti mphamvu kapena ulamuliro opatsidwa. Liwu loti “*dunamis*” limatanthauza kuti mphamvu zochibadwidwe. “Mphamvu zachibadwidwe” zimachokera malingaliro ndi mwaumwini. Mphamvu zachibadwidwe (*dunamis*) zagwiritsidwa ntchito mu vesi imeneyi pofuna kuwonetsa mphamvu za satana. Mphamvu zopatsidwa (*exousia*) zagwiritsidwa ntchito kufuna kuwonetsa mphamvu za Yesu zomwe anapatsidwa ndi Mulungu. Ndi mphamvu zolandira kuchokera kwa Mulungu zomwe ziri zoposa mphamvu ya mdani. Mphamvu zopatsidwa ndi zomwe zinaperekedwanso kwa okhulupirira. Inu simunabadwe ndi mphamvu. Simunatengerenso mphamvuzi kwa makolo anu. Koma zinapatsidwa kwa inu ndi Yesu Kristu.

UDINDO PA MPHAMVU

Mphamvu zomwe Yesu anapatsa ophunzira Ake zinaperekedwa ndi cholinga chapaderadera. Zimayenera kugwiritsidwa ntchito pofalitsira Uthenga Wabwino ku maiko onse.

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Machitidwe 1:8)

Mphamvu zimene cholinga chake ndi kufakiritsa Uthenga Wabwino ku maiko onse.

Yesu ananena fanizo pofotokoza chowonadi chenimenechi pa Marko 13. Anati:

Monga ngati munthu wa paulendo, adacoka kunyumba kwace, nawapatsa akapolo ace ulamuliro, kwa munthu ali yense nchito yace, nalamulira wapakhomo adikire. (Marko 13:34)

Ulamuliro unaperekedwa ndi cholinga chokakwaniritsa ntchito. Ntchito imeneyi ndi kufalitsa Uthenga Wabwino kufikira kumaiko onse.

KODI ZINALI ZAKALE?

Anthu ena amanena kuti kudzadzidwa kumeneku ndi mphamvu ya Uzimu kunali kwa mpingo woyamba kokha basi. Amanena kuti zinali za ophunzira a Yesu okha basi. Amenena kuti masiku azozizwa anali akale.

Koma talingalirani funso iri. Kodi dziko lonse lapansi lafikiridwa ndi Uthenga Wabwino? Ntchito yomwe Yesu anasiya kwa ophunzira Ake sinamalizike. Tinakalibe ndi udindo ofikira dziko lapansi ndi Uthenga Wabwino wa ufumu wa Mulungu. Yesu sadzachotsa ulamuliro ntchito ndi udindo usanakwaniritsidwe.

Werengani za imfa ndi chiukitso cha Lazaro mu Yohane 11. Yesu anafika pamene Lazaro atamwalira kale, Mariya anakumana naye Iye ndipo anati:

Ndipo Marita anati kwa Yesu, Ambuye, mukadakhala kuno mlongo wanga sakadafa. (Yohane 11:21)

Yesu anati kwa iye:

Yesu ananena naye, Mlongo wako adzauka. (Yohane 11:23)

Marita anati:

Marita ananena ndi iye, Ndidziwa kuti adzauka m'kuuka tsiku lomariza. (Yohane 11:24)

Kenako Yesu anati kwa iye:

Yesu anati kwa iye, Ine ndine kuuka ndi moyo; wokhulupirira Ine, angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo; Yohane 11:25

Marita amakhulupira kuti Yesu anakatha kumuukitsa Lazaro mbuyo (“... munakakhala kuno). Anakhulupiriranso kuti Yesu azamuukitsa iye mtsogolo (patsiku lomaliza). Koma Yesu anagawana naye chowonadi chofunikwa kwambiri. Anati “Ine Ndine” kuunika ndi moyo. “Ine Ndine” akunena za nthawi yapano. Ndipo kenako anamuukitsa Lazaro.

Palibe kuti zozizwa zinachitika kale masiku akale. Palibeso kuti zizachitika mtsogolo. Panthawi ina iliyonse pamakhala mphamvu yokuti chozizwa chitha kuchitika ndi cholinga chokumana ndi zosowa za anthu. Patsiku lilironse ndi m’badwo uliwonse, Mulungu amawonetsera mphamvu Yake. Akuyakhula kwa inu, “Ine Ndine”—nthawi yatsopano.

MOYO KUCHOKERA KUMPESA

Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zace: wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala cipatso cambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kucita kanthu. (Yohane 15:5)

Kudziko la kunthupi, moyo umachokera ku mpesa. Mpesa umatumiza moyo kunthambi kuti zikabereke chipatso. Nthambi simabereka chipatso payokha. Koma ngati yalekenatsidwa ndi tsinde la mpesa, imaleka kuberaka chipatso ndipo kenako imafa.

Yesu anaperaka chitsanzo chimenechi kuti awonetsere mmene mphamvu ya Mulungu imayendera mu dziko la Uzimu. Ife ndi nthambi zomwe zimabereka chipatso. Yesu ndi mpesa. Simupanga chipatso, koma mumangobereka chabe (onani Yohane 15)

chozizwa champhamvu munthawi ya Chipangano Chatsopano sichinali chozizwa cha Petro. Sinali ntchito ya manja a Paulo. Chinali chotsatira chamoyo wa Mulungu umene umayenda mwa iwo monga nthambi za Uzimu zopereka chipatso cha Uzimu.

Anthu awa anapanga zomwe Mulungu anawalamula. Analalikira mau. Anasanjika manja pa odwala. Analamula ziwanda kutuluka. Anamvera ndipo anasiya zotsatira mmanja mwa Mulungu.

Kumvera Mulungu ndikusiya zotsatira mmanja Mwake. Inu siwochita zozizwitsa. Mulungu nde chiyambi cha mphamvu. Pamena mukumvera Mulungu, ndi kuchita pa mau Ake, ziri kwa Iye kutulutsa mphamvu kudzera mwa inu.

Pamene ophunzira anafunsa “Tichite chiyani, kuti tichite ntchito ya Mulungu?” Yesu anayakha...

Yesu anayankha nati kwa iwo, Nchito ya Mulungu ndi iyi, kuti mukhulupirire iye amene Iyeyo anamtuma. (Yohane 6:29)

Yesu ndi mene amagwira ntchito kudzera mwa inu. Ndi amene wapereka ulamulilo. Simukuyenera kugwiritsa ntchito mphamvu ndi maganizidwe anu. Simukuyenera ku “ichepsya”. Ndi mphamu ya Mulungu imene ikugwira ntchito mwa inu ndikudzera mwa inu:

Ndipo iwowa anaturuka, nalalikira ponse ponse, ndipo Ambuye anacita nao pamodzi, natsimikiza mau ndi zizindikilo zakutsatapo, Amen. (Marko 16:20)

Nthawi zambiri mu utumiki ndondomeko imeneyi imasephanitsidwa. Ambiri ayesera kumugwirira ntchito Mulungu. Koma dondomeko yobweretsa zotsatira zamphamvu ndiyakuti “Mulungu amagwira ntchito ndi iwo.”

ZOLINGA

Anthu sanangopereka mphamvu kwa ena pokhapokha ngati ali ndi cholinga chochitira choncho. Nthawi zonse pamakhala cholinga pamene ulamuliro ukuperekedwa.

Mwaphunzira mu chaputala chino cholinga chachikulu cha mphamvu ya uzimu kuti ndi kufuna kupitsa pamtsogolo Uthenga Wabwino. Koma palinso zolinga zina zofunikira zopereka ulamuliro. Muphunzira zolinga zamphamvu zimenezo mu chaputala chotsatira.

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Kodi okhulupirira amalandira mphamvu kuchokera kwandani?

3. Kodi pali ngwirizano wotani pakati pa udindo ndi ulamuliro?

4. Kodi udindo waukulu womwe Yesu anapereka kwa ophunzira Ake unali wotani?

5. Pali mau awiri a Chigriki amene amagwiritsidwa ntchito kukamaba za mphamvu.

Kodi liwu loti “dunamis” limatanthauza chani? _____

Kodi liwu loti “exousia” limatanthauza chani? _____

6. Kodi kunena uku mkowona kapena konama?

“zozizwa zimkachita kale. Lero tiribe kuonetsera kwamphamvu kumene ophunzira a Yesu anakuona.”

Kunena uku ndi _____

(Mayankho amayesowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli.)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Werengani buku la Machitidwe kuti muone mmene ophunzira anakwanitsira udindo ndi mphamvu zomwe anapatsidwa ndi Yesu.

Lembani malemba omwe akuonetsa machitidwe amphamvu ya Mulungu mu kolamu yoyamba. Lembani mwachidule zomwe zinachitika mukolamu yachiwiri. Mukolamu yachitatu, fotokozani zotsatira zake za mphamvu ya Mulungu. Chitsanzo chaperekedwa kwa inu kuti mutsatire.

Machitidwe	Mmene mphamvu ya Mulungu	zotsatira
Ndime	inaonetsedwera	
Machitidwe 2 anali	Kuperekedwa kwa Mzimu Woyera	Petro yemwe poyamba
umboni		Wamantha, anachitira
miyoyo		Omwe usapulumsa
		Zikwi zitatu (3000)

CHAPUTALA 6

CHOLINGA CHA MPHAMVU

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Ksogolera kulemba vesi yotsogolera osawonera.
- Kufotokoza kusiyana kwa mphamvu ya uzimu ndi mphamvu yakunthupi.
- Kupereka umboni wamalemba omwe umatsimikiza kuti ndondomeko za dziko ndizosiyana kwambiri ndi ndondomeko za mu ufumu wa Mulungu.
- Kuwonetsera cholinga cha mphavu ya uzimu.

VESI YOTSOGOLERA:

Ndipo iwowo anaturuka, nalalikira ponse ponse, ndipo Ambuye anachita nao pamodzi natsimikiza mau ndi zizindikiro zakutsatapo.(Marko 16:20)

MAU OYAMBA

Mphamvu zosatsogozedwa bwino zikhoza kukhala zoopsya. Mphamvu ya mtsinje wamphamvu kwambiri ikhoza kutsogoleredwa ku zolinga zabwino komanso mtsinje ukhoza kubweretsa madzi kwa alimi. Sitima zazikulu kwambiri zikhoza kumayendapo. Madera mwina akhoza kumagwiritsa ntchito kupanga mphamvu za“magetsi.”

Koma mtsinje omwewo, ngati sutsogoleredwa, ukhoza kusefukira mkuwononga kwambiri. Ukhoza kuwonga mbeu ndi malo, kugwetsa nyumba, komaso ukhoza kuchotsa miyoyo. Umenewo ukhoza kukhala mtsinje womwewo. Mtsinje umakhala wabwino ngati utsogoleredwa kucholinga chabwino, ndipo umawonga ngati sutsogoleredwa.

Mphamvu za uzimu zogwiritsidwa ntchito cholinga cholakwikwa ndizoopsya monga ngati mtsinje wamphamvu kwambiri omwe sunatsogoleredwe bwino. Nde pachifukwa ichi mkwabwino kumvetsa bwino chomwe malemba amanena pa zolinga za mphamvu ya uzimu.

ZOLINGA ZAKUNTHUPI

Monga momwe mwaphunzira kale pachiyambi penipeni paphunziro lino, kuti pali mitundu yambiri ya mphamvu yomwe ikugwira ntchito pa dziko lero.

Mphamvu zandale zimagwiritsidwa ntchito pofuna ulamuliro wabungwe, mtundu, mudzi, mzinda, mdera ndi dziko lonse.

Mphamvu ya nzeru imagwiritsidwa ntchito yopeza zinthu zatsopano, kuwerenga ndi kupanga nyimbo, ndikukhazikitsa sukulu zambiri.

Mphamvu yakunthupi imagwiritsidwa ntchito pofuna kupanga pa masewero osiyanasiyana pano padziko.

Mphamvu ya chuma imapanga phindu lalikulu pazamalonda, komaso imakhazikitsa ufumu wazachuma.

Mphamvu ya asilikali imagwiritsidwa ntchito poteteza komaso kukuza malire.

Mphamvu ya zamphamvu imamuthanidza munthu munjira zambiri kuyambira pakamoto kochepa kongozitethetsera kufikira kumagetsi omwe amatumikira mzinda onse.

Mphamvu ya chipembedzo imapanga matchalitchi akuluakulu ndi timagulu tazipembedzo tochuluka.

Koma mwazonsezi palibepo zolinga za mphamvu zomwe Baibulo limafotokoza.

OSATI MONGA AMITINDU

Panthawi ina mmene Yesu amkaphunzitsa ophunzira ake zokhudzana ndi utsogoleri, Anati:

Koma Yesu anawaitana, nati, Mudziwa kuti mafumu a anthu amadziyesa okha ambuye ao, ndipo akuru ao amacita ufumu pa iwo. Sikudzakhala comweco kwa inu ai; koma amene ali yense akafuna kukhala wankuru mwa inu, adzakhala mtumiki wanu; ndipo amene ali yense akafuna kukhala woyamba mwa inu, adzakhala kapolo wanu: (Mateyu 20:25-27)

Yesu amkaphunzitsa ophunzira Ake ndodomeko yofunika kwambiri yomwe itha kugwira ntchito mmalo ambiri mmoyo pambali pa utsogoleri. Mau oti “Amitundu” amagwiritsidwa ntchito pofuna kutchula anthu ndi maiko omwe asiyanitsidwa ndi Mulungu. Yesu anafotokoza kuti ufumu wa Mulungu umagwira ntchito pandondomeko zomwe ziri zosiyaniranatu ndi ndondomeko za dziko lino.

Ndondomeko zimenezi zimagwiraso ntchito chimodzimidzi pamene tikukakamba za mphamvu. Zolinga zamphavu za dziko ndizosiyna ndi zolinga za mphamvu mu Ufumu wa Mulungu.

Mphamvu zimagwiritsidwa ntchito pa zolinga zozikonda pano pa dziko lapansi. Mu Ufumu wa Mulungu, pamene mu Ufumu wa Mulungu, mphamvu imagwiritsidwa ntchito pa zolinga zosazikonda pofuna kukuza Ufumu.

Anthu ena amagwiritsa ntchito mphamvu ya Uzimu molakwikwa ndipo amaigwiritsa ntchito pokhazikitsa zipembedzo ndi matchalitchi ambiri. Amaigwiritsa ntchito pokhazikitsa ufumu wazachuma ndiposo pofuna kuti atchuke. Koma izi sizolinga za mphamvu ya Uzimu zomwe ziri Mmalemba. Anthu oterewa akusokoneza cholinga cheni cheni chomwe Yesu anaperekeramulamuliro kwa okhulupirira. Alembi ndi Afalisi mu Chipangano Chatsopano ndi zitsanzo za kagwiritsidwe ntchito kolakwika ka mphamvu ya Uzimu. Yesu anati:

Tsoka inu, Afalisi! cifukwa mukonda mipando yaulemu m' masunagoge, ndi kulankhulidwa m' misika. Tsoka inu! cifukwa muli ngati manda osaoneka, ndipo anthu akuyendayenda pamwamba pao sadziwa, (Luka 11:43-44)

Alembi ndi Afalisi anali atsogoleri amphamvu achipembedzo. Amkagwiritsa ntchito mphamvu imeneyi kuti apindule iwo eni. Amakhala pamipando yabwino ma Sunagoge. Amafuna kupatsidwa moni wapaderadera misika. Amkagwiritsaso mphamvu zawo potsekera anthu:

Koma tsoka inu, alembi ndi Afalisi, onyenga! cifukwa mutsekera anthu Ufumu wa Kumwamba pamaso pao; pakuti inu nokha simulowamo, Ndipo muwaletsa amene alikulowa, kuti asalowemo. [(Mateyu 23:13)

Tsoka inu, alembi ndi Afalisi, onyenga! cifukwa mupitapita kunyanja ndi kumtunda kuyesa munthu mmodzi mtembenuki; ndipo m' mene akhala wotere, mumsandutsa mwana wa gehena woposa inu kawiri. (Mateyu 23:15)

Afalisi amawonetsera kwambiri kunja mphamvu yawo yachipembedzo, koma amagwiritsa ntchito pofuna kuti iwo apindule:

Koma tsoka inu, alembi ndi Afalisi, onyenga! cifukwa mutsekera anthu Ufumu wa Kumwamba pamaso pao; pakuti inu nokha simulowamo, Ndipo muwaletsa amene alikulowa, kuti asalowemo. [(Mateyu 23:14)

Anali ndi mphamvu ya chipembezo, koma analibe mphamvu yeniyeni ya uzimu. Yesu anati anali ngati manda osawaka, akufa kwenikweni ndiposo opanda mphamvu omwe anthu amatha kumayenda pamutu pawo koma iwo osazindikira.

ZOLINGA ZA MPHAMVU ZA M'BAIBULO

Izi ndi zolinga za mphamvu ya Uzimu zomwe ziri m'Baibulo:

CHIPULUMUTSO:

Cholinga choyamba cha mphamvu ya Uzimu ndi chipulumutso:

Koma onse amene anamlandira iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lace; (Yohane 1:12)

Pakuti mau a mtanda ali ndithu cinthu copusa kwa iwo akutayika, koma kwa ife amene tirikupulumutsidwa ali mphamvu ya Mulungu. (1 Akorinto 1:18)

Zotsatira pakuwonetseredwa kwa mphamvu ya Mulungu ndi chipulumutso. Midzi ya Luda ndi Saroni inatembenuka pamene Eneya, wamanjenje amene anagona kwa zaka zisanu ndi zitatu anachiritsidwa (Machidwe 9).

KUCHITIRA UMBONI:

Cholinga chachikuli chomwe mphamvu ya Uzimu inaperekedwera kwa okhulupirira chinanedwa pamene Yesu amkalonjeza za mphamvu imeneyi:

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Machitidwe 1:8)

Muphunziro zambiri zokhudza mphamvu ya Mzimu Woyera patsogolo mu phunziro lino.

Mphamvu zomwe Yesu anapereka kwa Ophunzira Ake zinayenera kubwera pa iwo Mzimu Woyera akafika. Cholinga cha mphamvu chinali kufuna kupititsa patsogolo kuchitira umboni Uthenga wabwino, kuyambira mu Yerusalemu ndi kukafika kumalekezero kwa dziko lapansi.

Kuwonetsera koyamba kwa mphamvu ya Uzimu inemeyi kunawonekera koyamba mwa mtumwi Petro. Atalandira Mzimu Woyera, anapereka umboni wa mphamvu wa Uthenga Wabwino omwe unapangitsa kuti anthu okwana zikwi zitatu apulumutsidwe. Ameneyu anali Petro yemwe uja anathawa Yesu atamagwidwa. Ameneyu ndi Petro yemwe uja amene anakana kuti samudziwa Ambuye Yesu. Nde chinachitika ndi nchani?

Petro anadzadzidwa ndi mphamvu ya Uzimu. Anakumbukira cholinga cha mphamvu imeneyi monga mmene ananenera Yesu, “Muzakhala mboni Zanga.” Pamene analandira mphamvu anayamba kuigwiritsa ntchito moyenera pofalitsa Uthenga wabwino kwa amuna ndi akazi osapulumsidwa.

Mubwalo la milandu, “umboni” umakhala ndi mbali ziwiri; umboni wapakamwa ndi umboni wowoneka. Chowonadi ichi chirinso chimodzimodzi mu dziko la Uzimu. Pochitira umboni za Uthenga Wabwino tikuyenera kukhala ndi umboni wongoyakhula komaso wowoneka.

Zowoneka ndiko kuwonetsera mphamu ya Mulungu:

Ndipo atumwi anacita umboni ndi mphamvu yaikulu za kuuka kwa Ambuye Yesu; ndipo panali cisomo cacikuru pa iwo onse. (Machitidwe 4:33)

Paulo analemba:

kuti Uthenga Wabwino wathu sunadza kwa inu m'mau mokha, komatunso mumphamvu, ndi mwa Mzimu Woyera, ndi m'kucuruka kwakukuru; monga mudziwa tinakhala onga otani mwa inu cifukwa ca inu. (1 Atesalonika 1:5)

Yesu analonjeza kugwira ntchito ndi onse amene amvera lamulo lopita kudziko lapansi kukachitira umboni kwa zolengedwa zonse. Anthu ena amasaka zizindikiro zamphamvu mu utumiki wawo, pamene sakukwaniritsa lamulo lopita. Mphamvu zomwe Yesu analonjeza ndi za okhawo amene akukwaniritsa lolamulo.

KULIMBA MTIMA:

Pakuti Mulungu sanatipatsa mzimu wa mantha; komatu wa mphamvu ndi cikondi ndi cidziletso. (2 Timoeo 1:7)

Mu mpingo woyamba Uthenga Wabwino unalalikidwa molimbika mtima chifukwa chakudzadzidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera,

Ndipo m'mene adapemphera iwo, panagwedezeka pamalo pamene adasonkhanirapo; ndipo anadzadzidwa onse ndi Mzimu Woyera, nalankhula mau a Mulungu molimbika mtima. (Machitidwe 4:31)

Koma Bamaba anamtenga, napita naye kwa atumwi, nawafotokozerera umo adaonera Ambuye m'njira, ndi kuti analankhula naye, ndi kuti m'Damasiko adanena molimbika mtima m'dzina la Yesu. (Machitidwe 9:27)

(Machitidwe 18:26)

ndipo iye anayamba kulankhula molimba mtima m'sunagoge, koma pamene anamumva iye Priskila ndi Akula, anamtenga, namfotokozerera njira ya Mulungu mosamalitsa. (Machitidwe 19:8)

Atesalonika 2:2 koma tingakhale tidamva zowawa kale, ndipo anaticitira cipongwe, monga mudziwa, ku Filipi, tinalimbika pakamwa mwa Mulungu wathu kulankhula ndi inu Uthenga Wabwino wa Mulungu m'kutsutsana kwambiri. (1 Atesalonika 2:2)

KUGWIRA NTCHITO ZA MULUNGU:

Ophunzira anazizwa ndi ntchito zaphamvu zomwe Yesu anachita:

Ndipo Iye anaturuka kumeneko; nafika ku dziko la kwao; ndipo ophunzira ace anamtsata. Ndipo pofika dzuwa la Sabata, anayamba kuphunzitsa m'sunagoge; ndipo ambiri anamva Iye, nazizwa, nanena, Uyu adazitenga kuti izi? Nzeru yopatsidwa kwa munthuyu njotani, ndi zamphamvu zotere zocitidwa ndi manja ace? (Marko 6:1-2)

Yesu anati:

Tiyenera kugwira nchito za iye wondituma Ine, pokhala pali msana; ukudza usiku pamene palibe munthu angakhoze kugwira nchito, (Yohane 9:4)

Yesu anali ndicholinga cheni cheni: Amayenera kugwira ntchito za Mulungu. Ichi ndichimene chinali chomutakasa Chake. Atachitira umboni ntchito zimenezi kwa nthawi, ophunzira anabwera kwa Yesu ndi funso:

Pamenepo anati kwa iye, Ticite ciani, kuti ticite nchito za Mulungu? (Yohane 6:28)

Yesu anayakha:

Yesu anayankha nati kwa iwo, Nchito ya Mulungu ndi iyi, kuti mukhulupirire iye amene Iyeyo anamtuma. (Yohane 6:29)

Ntchito yaikulu ya Mulungu inawonetseredwa mwa Yesu. Ambuye chidwi chawo chinali pa ophunzira Awo kusiyana kungowonetsa zizindikiro ndi zozizwa. Zozizwa zenizeni nthawi zonse zimamukweza Yesu. Iyi nde ntchito ya Mulungu.

Yesu anawauza ophunzira Ake:

Indetu, indetu, ndinena kwa inu, Wokhulupirira Ine, nchito zimene ndicita Ine adzazicitanso iyeyu; ndipo adzacita zoposa izi; cifukwa ndipita Ine kwa Atate. (Yohane 14:12)

Ophunzira Ake amkayenera kuchitaso chimodzi modzi ntchito imene Iye anachita. Anachita ntchito yopambana. Ntchito zimenezi zinayenera kukhala zochuluka. Lonjezano lake linakwaniritsidwa, kupyolera mu buku la Machitidwe limene limachitira umboni za ophunzira akuchita ntchito ya Mulungu. Odwala akuchiritsidwa, ziwanda zikutulitsidwa, zitseko zandende zikutsekulidwa, ndiposo akufa akubwezeretsedweraso moyo.

KUWONETSERA MULUNGU:

Mwaphunzira kuti cholinga chimodzi chimene Mulungu amawotsera mphamvu Yake pano padziko ndikufuna kuziwonetsera Yekha kwa munthu. Mphamvu ya Uzimu imene inaperekedwa kwa okhulupirira inali ndi cholinga ngati chomwechi:

Ndipo m'mene anthu a makamu anaciona, anaopa, nalemekeza Mulungu, wakupatsa anthu mphamvu yotere. (Mateyu 9:8)

Kupyolero mu Eklezia wa mphamvu, Mulungu amafuna kuziwulula Yekha ku dziko lonse:

kuti mu Eklesia azindikiritse tsopano kwa akulu ndi maulamuliro m'zakumwamba nzeru ya mitundu mitundu ya Mulungu, (Aefeso 3:10)

Cholinga chabvumbulutso iri kudzera mumphamvu ndi:

Ndipo anacita coteru masiku ambiri. Koma Paulo anabvutika mtima ndithu, naceuka, nati kwa mzimuwo, Ndikulamulira iwe m'dzina la Yesu Kristu, turuka mwa iye. Ndipo unaturuka nthawi yomweyo. (Machitidwe 26:18)

KUWONETSERA UFUMU WA MULUNGU:

Yesu anamphatikiza kulalikira ufumu wa Mulungu ndi kuwonetsera kwake komwe. Pamene Yesu anafunsidwa “Kodi ndinu wakudzayo” (Luka 7:19), sanayakhe ayi. Anati :

Ndipo anayankha, nati kwa iwo, Mukani, muuze Yohane zimene mwazona, nimwazimva; anthu akhungu alandira kuona kwao, opunduka miyendo ayenda, akhate akonzedwa, ogontha akumva, akufa aukitsidwa, kwa aumphawi ulalikidwa Uthenga Wabwino. (Luka 7:22)

Mphamvu zimawonetsera Ufumu wa Mulungu uli kuchitachita. Zozizwa za Yesu zinawonetsa kuti Ufumu wa Mulungu unali utafika. Anawonetsera mmene Ufumu umakhalira ukamazawoneka ndimaso kumwamba kwatsopano ndipameneso dziko lapansi latsopano lizalengedwe:

- Kutulutsa ziwanda ndi chizindikiro cha Mulungu kuti walowerera maukulu a satana ndi chiwonongeko chachimaliziro chake chatsala pang'ono: Mateyu 12:29; Marko 3:27; Luka 11:21; Yohane 12:31; Chibvumbulutso 20:1
- Kuchilitsidwa kwa odwala kumawonetsera za tsiku lomwe mazuzo onse azanthe: Chibvumbulutso 21:4
- Chakudya cholandirinda munjira ya chozizwa zimanena za tsiku lomwe zonsewa za anthu zinzatheretu: Chibvumbulutso 7:1
- Kutonthoza namondwe zimawonetsera za tsiku lachingonjetso pa mphamvu zomwe zimagwiritsa ntchito chilengedwe powopsyeza dziko lapansi: Chibvumbulutso 21:1
- Kudzutsa akufa zimalengeza kuti imfa tsiku lina idzathedwa: 1 Akorinto 15:26

KUPEREKA CHITSIMIKIZO CHA MAU:

Zizindikiro za mphamvu ndi zodabwitsa ndi chitsimikizo cha Mau a Mulungu:

Cifukwa cace anakhala nthawi yaikuru nanenetsa zolimba mtima mwa Ambuye, amene anacitira umboni mau a cisomo cace, napatsa zizindikiro ndi zozizwa kuti zicitidwe ndi manja ao. (Machitidwe 14:3)

Ndipo tsopano Ambuye, penyani mau ao akuopsa, ndipo patsani kwa akapolo anu alankhule mau anu ndi kulimbika mtima konse, m'mene mutambasula dzanja lanu kukaciritsa; ndi kuti zizindikilo ndi zozizwa zicitidwe mwa dzina la Mwana wanu wopatulika Yesu. (Machitidwe 4:29-30)

Ndipo iwowa anaturuka, nalalikira ponse ponse, ndipo Ambuye anacita nao pamodzi, natsimikiza mau ndi zizindikilo zakutsatapo, Amen. (Marko 16:20)

UTUMIKI KWA ENA:

Mphamvu ya Mulungu inali pa Yesu kuti ikamukozekeretse ku utumiki:

ndipo mzimu wa Yehova udzambalira iye mzimu wanzeru ndi wakuzindikira, mzimu wa uphungu ndi mphamvu, mzimu wakudziwa ndi wakuopa Yehova; (Yesaya 11:2)

Mzimu wa Ambuye Yehova uli pa ine; pakuti Yehova wandidzoza ine ndilalikire mau abwino kwa ofatsa; Iye wanditumiza ndikamange osweka mtima, ndikalalikire kwa am'nsinga mamasulidwe, ndi kwa omangidwakitsegulidwa kwa m'ndende; (Yesaya 61:1)

za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Machitidwe 10:38)

Ndipo anazizwa ndi ciphunzitso cace; pakuti anaphunzitsa monga mwini mphamvu, si monga alembi. (Marko 1:22)

Mphamvu yomweyi inachitiridwa umboni mu utumiki wa okhulupirira mu mpingo woyamba.

Paulo anati:

umene anandikhalitsa mtumiki wace monga mwa mphatso ya cisomo ca Mulungu, cimene anandipatsa ine, monga mwa, macitidwe a mphamvu yace. (Aefeso 3:7)

Mphamvu ya Mulungu yomwe ikugwira ntchito mwa inu izakupangitsani kuti muyambe kutumikira. Utumiki wanu umabadwa ndikumakula chifukwa cha mphamvu ya Mulungu yomwe ikugwira ntchito mwa inu. Paulo anati:

Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'cionetso ca Mzimu ndi ca mphamvu; kuti cikhulupiriro canu cisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu. (1 Akorinto 2:4-5)

Mpingo woyamba unabadwa pakuwonetseredwa kwa mphamvu ya Mulungu, osati chifukwa choyakhula bwino kapena mkambirano wazokhudza Mulungu. Izi zinawapangitsa kuti chikhulupiriro chawo chikhazikike mwa Mulungu osati pakudziwa ndikuthekera koyakhula kwawo.

Mphamvu ya Mulungu imapangitsa kuti madera onse a uzimu zinthu izi zichitike: kufalitsidwa kwa Uthenga Wabwino, kutumikira kwa odwala, ndi onse amene amangidwa ndi nsinga zamphamvu ya ziwanda:

Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi. Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: (Mateyu 28:18-19)

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Marko 16:17-18)

Ndipo pamene Iye anadziitanira ophunzira ace khumi ndi awiri, anapatsa iwo mphamvu pa mizimu yoipa, yakuiturutsa, ndi yakuciza nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 10:1)

Munthu amavomerezedwa ngati mtumiki chifukwa cha mphamvu ya Mulungu:

koma m'zonse tidzitsimikfzira ife tokha monga atumiki a Mulungu, m'kupirira kwambiri, m'zisautso, m'zikakamizo, m'zopsinja, m'mau a coonadi, mu mphamvu ya Mulungu; mwa camuna ca cilungamo kulamanja ndi kulamanzere, (2 Akorinto 6:4, 7)

CHIFUKWA CHA NKHONDO YA UZIMU:

Pamene mukwaniritsa cholinga cha mphamvu pokuza Uthenga Wabwino, muzakumana ndi zotsutsa za satana. Yesu waperaka mphamvu kwa inu chifukwa cha nkondo ya uzimu. Wakupatsani mphamvu pamwamba pamphamvu zonse za mdani.

Taonani, ndakupatsani ulamuliro wakuponda pa njoka ndi zinkhanira, ndi pa mphamvu iri yonse ya mdaniyo; ndipo kulibe kanthu kadzakuipsani konse. (Luka 10:19)

Cotsalira, tadzilimbikani mwa Ambuye, ndi m'kulimba kwa mphamvu yace. Tabvalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kucirimika pokana macenjerero a mdierekezi. Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:10-12)

KUPEWA KULAKWITSA KWA UZIMU:

Anthu amapezeka kuti alakwitsa ku uzimu pazifukwa ziwiri:

Koma Yesu anayankha, nati kwa iwo, Mungolakwa a osadziwa malembo, kapena mphamvu za Mulungu. (Mateyu 22:29)

Kulakwita kuuzimu kumabwera chifukwa chosadziwa Mau a Mulungu chifukwa mumakhala kuti mwatsegula khomo lachinyengo ndi ziphunzitsa zobodza. Kulakwitsa kwa uzimu kumabwera chifukwa chosadziwa mphamvu ya Mulungu. Mumakhala kuti mwatsegulira khomo la mphamvu yonyenga ya mdaniyo. Inu makhala ovulazidwa ndi mphamvu imeneyi yomwe ikugwira ntchito mutsutsana nanu pamena mulibe mphamvu ya Uzimu yomwe imakaniza mphamvu yake.

akukhala nao maonekedwe a cipembedzo, koma mphamvu yace adaikana; kwa iwonso udzipatule, (2 Timoteo 3:5)

CHIGONJETSO PA TCHIMO:

Mphamvu ya Uzimu imabweretsa tchimo:

Pakuti ucimo sudzacita ufumu pa inu; popeza simuli a lamulo koma a cisomo. (Aroma 6:14)

KUMANGIRIRA:

Paulo anawalemba Akorinto:

Pakuti ndingakhale ndikadzitamandira kanthu kocurukira za ulamuliro (umene anatipatsa Ambuye ku kumangirira, ndipo si ku kugwetsera kwanu), sindidzanyazitsidwa; (2 Akorinto 10:8)

Cifukwa ca ici ndilembera izi pokhala palibe ine, kuti pokhala ndiri pomwepo ndingacite mowawitsa, monga mwa ulamuliro umene Ambuye anandipatsa ine wakumangirira, ndipo si wakugwetsa. (2 Akorinto 13:10)

Paulo anazindikira ulamuliro wake kuti sumayenera kugwiritsidwa ntchito pozusa anthu kapena kuwawonongaso. Iye anali ndi chizolowezi choyakhula mowawitsa, ndipo anawalemba Akorinto zokhudzana pankhani zovuta. Samafuna kugwiritsa ntchito udyo mphamvu za Uzimu zomwe Mulungu anampatsa iye. Mphamvu yochokera kwa Mulungu inaperekedwa kwa Paulo kuti akamangirire ena, osati kuwawononga. “Kumangirira” kumatanthauza kuti kupititsa patsogolo kukula kwa uzimu.

Izi sizitanthauza kuti tiribe mphamvu yopereka mwambo kwa omwe alakwitsa mkachisi. Ulamuliro wa Uzimu umapatsidwa kwa atsogoleri kuti apereke mwambo molingana ndi malamulo amene aperekedwa m’mau a Mulungu. Mpingo opanda mphamvu umakhala opanda mwambo konse.

KULENGA KOFUNITSITSA:

Munthu aliyense ali ndi maganizo ake. Maganizo amenewo ndi mphamvu ya kusankha. Kuwonetsera kwa mphamvu kumalenga kufunitsitsa kukhala omasuka kwa Mulungu:

Anthu anu adzadzipereka eni ace tsiku la camuna canu: M'moyera mokometsetsa, mobadwira tnatanda kuca, Muli nae mame a ubwana wanu. (Masalimo 110:3)

KUPANGITSA MULUNGU KUTI AGWIRE NTCHITO:

Mulungu amagwira ntchito moyenerana ndi mulingo omwe mwamuloreza kuti agwire ntchito mwa inu:

Ndipo kwa iye amene angathe kucita koposa-posatu zonse zimene tizipempha, kapena tiziganiza, monga mwa mphamvu ya kucita mwa ife, (Aefeso 3:20)

Chonse chimene mungamufuse Mulungu zonse zokhudzana ndi chilungamo cha uzimu chimakhudzidwa ndi mphamvu ya Mulungu imene ikugwira ntchito mwa inu.

KULIMBIKA KWA UZIMU:

Mphamvu ya Mulungu simphamvu chabe imene imangogwira ntchito kupyolera mwa inu, koma ndi mphamvu yokupanganibe inu. Paulo anati ndife...

olimbikitsidwa m'cilimbiko conse, monga mwa mphamvu ya ulemerero wace, kucitira cipiriro conse ndi kuleza mtima conse pamodzi ndi cimwemwe, (Akolose 1:11)

Mphamvu ya Mulungu imalimbikitsa munthawi yomavuta pamene mukufuna chipiriro muzowawa. Mukhoza kukhala ndi chimwemwe muzowawa zomwe mukukumana nazo chifukwa cha mphamu ya ulemerero Wake imene ikugwira ntchito mwa inu. Ichi ndi chifukwa chofunika kwambiri cha mphamvu Yake imene ikugwira ntchito mwa inu.

Ndipo ananena kwa ine, Cisomo canga cikukwanira; pakuti mphamvu yanga ithedwa m'ufoko. Cifukwa cace makamaka ndidzadzitamandira rriokondweratu m'maufoko anga, kuti mphamvu ya Kristu ikhale pa ine. (2 Akorinto 12:9)

KUTETEZA:

Mwasungidwa, kapena mwatetezedwa ndi mphamvu ya Mulungu, kufikira kumapeto kwa nthawi:

amene musungidwa ndi mphamvu ya Mulungu mwa cikhulupiriro, kufikira cipulumutso cokonzeka kukabvumbulutsidwa nthawi yotsiriza. (1 Petro 1:5)

CHIUKITSO:

Mukukhala kuthupi lomwe la imfa ngati Yesu sabwera nsanga ku dziko lapansi. Nde ndi mphamvu ya uzimu imene izadzutse thupi lanu kuchiukitso.

lifessedwa m'mnyozo, liukitsidwa m'ulemerero; lifessedwa m'cifoko, liukitsidwa mumphamvu; (1 Akorinto 15:43)

koma Mulungu anaukitsa Ambuye, ndiponso adzaukitsa ife mwa mphamvu yace. (1 Akorinto 6:14)

MOYO WAMUYAYA:

Mphamvu ya Mulungu imapereka moyo wosatha:

**pakuti amcitira umboni, Iwe ndiwe wansembe nthawi yosatha Monga mwa
dongosolo la Melikizedeke. (Ahebri 7:16)**

KWA ZINTHU ZONSE:

Zinthu zonse zimene ziri zokhudzana ndi moyo ndi chiyero zaperekedwa kwa inu kupyolera ku mphamvu ya Mulungu:

**Wodalitsika Mulungu ndiye Atate wa Ambuye wathu Yesu Kristu, iye amene,
monga mwa cifundo cace cacikuru, anatibalanso ku ciyembekezo ca moyo, mwa
kuuka kwa akufa kwa Yesu Kristu; (1 Petro 1:3)**

Taganizani za zinthu zambiri zomwe zimachitika mmoyo. Taganizani za makhalidwe amene amachitika mchiyero. Cholinga cha mphamvu Yake ndi kukupatsani zinthu zinthu zonse.

MAYESO ODZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Kodi mphamvu ya uzimu imasiyana bwanji ndi mphamvu yapadziko lapansi?

3. Perekani umboni wochokera mmalemba omwe umafotokoza kuti ndondomeko za mphamvu ya dziko lapansi ndi zosiyana ndi ndondomeko ya mphamvu ya Ufumu wa Mulungu.

4. Mwaphunzira zolinga zambiri za mphamvu mu phunziro lino. Lembani ndime yachidule yokamba mwachidule zomwe mwaphunzira zokhudana zolinga zitatu.

(Mayankho amafusowa aperekdwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Yesu anati okhulupirira azachita ntchito zimene Iye anachita. Werengani Mateyo, Marko, Luka, ndi Yohane. Lembani ndandanda wa ntchito zimene Yesu anagwira. Zimenezi ndi ntchito zimenso inu mungachite kupyolera mu mphamvu ya Mulungu.
2. Pansipa pali mndandanda wa zolinga za mphamvu zomwe zakambidwa mu chaputalachi. Sathulani mulingo wa uzimu wanu. Kodi muzolingazi, ndi ziti zomwe zikuwonekera m'moyo wanu ndi utumiki? Ikani chizindikiro chophatikiza (+) pambali pa zomwe zikuonekera m'moyo wanu. Ikani chizindikiro chochosera (-) pambali pa zomwe zikufunika zitaonekera.

Chipulumutso	Chipamabano pa tchimo
Kuchitira umboni	Kumangirira
Kulimbika mtima	Kukhala ofunitsitsa
Kuwonetsera Mulungu	Kulimbika kwa Uzimu
Kuwonetsera Ufumu wa Mulungu	Kuteteza
Kutsimikizira Ufumu wa Mulungu	Kuuka
Kutumikira ena	Moyo osatha
Nkhondo ya Uzimu	Zinthu zonse zokhudza moyo
Kupewa kulakwitsa kwa uzimu	

3. Davide amayakhula kawiri kawiri zokhudzana ndi ntchito ya Mulungu mu buku la Masalimo. Werengani malemba otsatirawa:

8:6; 9:1; 14:1; 26:7; 28:5; 33:4,15; 40:5; 46:8; 66:3,5; 71:17; 73:28; 75:1; 77:11;
78:4,7,11,32; 86:8; 92:4,5; 103:22; 104:13,24,31; 105:2,5; 106:13,22,35,39;
107:8,15,21,22,24,31; 111:2,4,6,7; 118:17; 119:27; 138:8; 139:14; 141:4; 143:5;
145:4, 5, 9, 10, 17

Lembani mwachidule zimwene mwaphunzira mu ndime zimenezi.

CHAPUTALA 7

NDONDOMEKO YA MPHAMVU 1: MPHAMVU YA UNTHENGA WABWINO

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziro ili mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osawonera.
- Kupereka tanthauzo la “Uthengo Wabwino”.
- Kupereka umboni wa m’malemba omwe umakamba mwachidule maziko eni eni a Uthenga Wabwino.
- Kufotokoza chifukwa chimene Uthenga Wabwino uli wamphamvu.
- Kuonetsera phindu la mphamvu ya Mwazi wa Yesu.
- Kuonetsera chikhulupiriro ngati chinthu chofunika kwambiri pofuna mphamvu ya Uthenga Wabwino.
- Kukumana ndi mphamvu ya Uthenga Wabwino.

VESI YOTSOGOLERA:

Pakuti Uthenga Wabwino sundichititsa manyazi; pakuti uli mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wakukhulupirira; kuyambira Myuda, ndiposo Mhelene.Aroma 1:16.

MAU WOYAMBA

Mwaphunzira kufunika kwa mphamvu mmoyo wanu. Nde mwapeza kuti kochokera mphamvu ndi Mulungu ndipo mwaphunzira za mphamvu yopatsidwa kwa Yesu. Mu chaputala chomaliza mwaphunzira mmene mphamvu ya Uzimu inaperekedwera kwa okhulupirira. Koma kodi mungalandire bwanji mphamvu imeneyi? Kodi mungaitenge bwanji kuti muigwiritse ntchito mmoyo ndi utumiki wanu? Ndi ndondomeko ziti za uzimu zoomwe zimagwira ntchito? Chaputala ichi chayamba ndi maphunziro ambiri otchedwa “Ndongomeko za mphamvu.”

UTHENGA WABWINO

Tikamakamba za Uthenga molinga ndi Baibulo, timakamba za Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ndi chipulumutso kudzera mwa Yesu Kristu. Maziko enieni a Uthenga Wabwino anakambidwa mwachidule ndi mtumwi Paulo:

Pakuti ndinapereka kwa inu poyamba, cimenenso ndinalandira, kuti Kristu anafera zoipa zathu, mongamwa malembo; ndi kuti anaikidwa; ndi kutianaukitsidwa tsiku lacityatu, monga mwa malembo; (1 Akorinto 15:3-4)

Maziko eni eni a Uthenga Wabwino amakhazikika kwambiri pa moyo ndi utumiki wa Yesu. Kuphatikizapo imfa Yake chifukwa chamachimo a anthu onse, kuikidwa kwake mmanda, ndikuuka kwakakufa malinga ndizolembedwa zomwe zili m' mau a Mulungu. Muli mphamvu yopambana mu Uthenga Wabwino. Paulo anati:

Uthenga Wabwino sundicititsa manyazi; pakuti uti mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wakukhulupira; kuyambira Myuda, ndiponso Mhelene. Pakuti m'menemo caonetsedwa cilungamoca Mulungu cakucokera kucikhulupiro kuloza kucikhulupiro: monga kwalembedwa, Koma munthu wolungama adzakhala ndi moyo ndi cikhulupiro. (Aroma 1:16-19)

Vesi imeneyi imawonetsera chifukwa chomwe Uthenga Wabwino uli wamphamvu. Ndiwamphamvu chifukwa:

- Ndi bvumbulutso la mphamvu ya Mulungu kwa munthu.
- Umabweretsa chipulumutso kwa anthu onse, mosayang'ana mtundu, khungu kapena kochokera.
- Umailula zonse zokhudza Mulungu kwa anthu onse.
- Umailula chilango ndi mkwiyo wa Mulungu pa tchimo.
- Umawonetsera chipangamo cha Mulungu.
- Umawonetsera mmene tingalungamitsidwire mwa chikhulupiro.
- Ndi maziko achikhulupiro chomwe ife tikukhalira moyo.

MPHAMVU MU MWAZI

Mtanda ndi chida chobweretsa imfa, chinthu chopangidwa ndi mtengo ndipo Yesu ana ferapo. Mphamvu ya uthenga wabwino ndi yosasiyanitsidwa ndi mphamvu ya mtanda ndi mwazi umene unakhetsedwapo.

Mphamvu ya mtanda siri mu chinthu chopangidwa ndi mtengocho. Mphamvu siri muchifanifani chirichonse cha mtanda chomwe timavala kapena kuika pa makachisi athu. Mphamvu ya mtanda iri pazomwe zinachitika pa mtandapo. Ndi mwazi wa Yesu umene unakhetsedwa pa mtanda chifukwa cha machimo a anthu onse.

Baibulo limaphunzitsa kuti moyo wa munthu uli mwazi (Levitiko 17:11, 14). Chifukwa chilango cha tchimo ndi imfa (Aroma 6:23), nde pakuti moyo uli mwazi, Mulungu anakhazikitsa ndondomeko zakukhululukira machimo kumene kumachitika pakukhetsa mwazi.

Ndipo monga mwa cilamulo zitsala zinthu pang'ono zosayeretsedwa ndi mwazi, ndipo wopanda kukhetsa mwazi kulibe kumasuka. (Ahebri 9:22)

Muchipangano Chakale, mwazi wa nyama umaperekedwa msembe chifukwa cha tchimo. Kupereka msembe ya mwazi kumachitika kawiri kawiri pamene munthu wachimwa. Koma mu Chipangano Chatsopano, Mulungu anatumiza Yesu kuti azakhetsa mwazi chifukwa cha tchimo kamodzi ndi komaliza. Sikofunikaso kuti mwazi wa nyama uziperekedwa ngati msembe ya machimo.

kapena mwa mwazi wa mbuzi ndi ana a ng'ombe, koma mwa mwazi wa iye yekha, analowa kamodzi ku malo opatulika, atalandirapo ciombolo cosatha. (Ahebri 9:12)

Mphamvu ya mtada iri mu mwazi wa Yesu. Ndi mphamvu ya Uzimu yotani imene iri mwazi? Mwazi:

- Unakhetsedewa chifukwa chachikhululukiro cha machimo kwa anthu ambiri: Mateyu 26:28
- Unabweretsa chiombolo cha chamachimo kwa ife: Aefeso 1:7; 2:13; 1 petro 1:2, 18-19; Chibvumbulutso 5:6-9
- Ndi wantengo wapatali, chifukwa unatiwombola ife: 1 Petro 1:18-19
- Unayeretsa machimo anthu: 1 Yohane 1:7
- Unagula chikumbumtima chanthu ku tchimo: Ahebri 9:14

- Umatiyakhulira. Yesu ndi otimbedzera wathu ndipo mwazi Wake umatiyakhulira ife: Ahebri 12:24
- Umatipatsa mwayi okamufikira pamaso pa Mulungu: Ahebri 9:12; 10:19-22; Aefeso 2:13
- Umampanga Yesu kukhala nkhalapakati pa Mulungu ndi munthu: Ahebri 12:24
- Unatiyeretsa ife: Ahebri 13:12-13
- Ndi njira yolungamitsidwira: Aroma 3:24-25
- Ndi chikho cha madalitso auzimu: 1 Akorinto 10:16
- Unatiwombora ku tchimo ndi matenda: Yesaya 53:4
- Umaikira umbuyo ndi malonjezano a Kristu. Pamene Yesu anatenga chikho cha vinyo ndipo anati “Chikho ichi ndi pangano la mwazi Wanga” anana kuti “Lonjezo lirironse limene liri mu pangano lizasungidwa pa mtengo wa mwazi wamoyo Wanga”: Luka 22:20
- Ndi mphamvu imene iri kumbuyo kwa chiukitso cha Yesu: Ahebri 13:20
- Umabweretsa moyo: Yohane 6:53-57
- Umatipangitsa ife kukwaniritsa kuchita chifuniro cha Mulungu: Ahebri 13:20-21
- Umatipangitsa ife kuthekera kopambana mphamvu ya mdani: Chibvumbulutso 12:11
- Umapereka chitetezo: pamene mwazi wa pasaka wa nkhonsa unaikidwa pamwamba pa khomo la Aisraeli ku Aigupto, choipa sichinakalowa: Eksodo:12:21-23

Izi ndi chifukwa chimene Paulo anati:

Pakuti mau a mtanda ali ndithu cinthu copusa kwa iwo akutayika, koma kwa ife amene tirikupulumutsidwa ali mphamvu ya Mulungu. (1 Akorinto 1:18)

NDICHISAKHO

Pamene Yesu anapachikidwa pa mtanda, kodi izi zimatanthauz akuti adani Ake anali ndi mphamvu zambiri kuposera zomwe Iye anali nazo? Werengani zomwe Baibulo limalembe zokhudza zimenezi:

Cifukwa cace Pilato ananena kwa iye, Simulankhula ndi ine kodi? simudziwa kodi kuti ulamuliro ndiri nao wakukumasulani, ndipo ndiri nao ulamuliro

wakukupacikani? Yesu anamyankha iye, Simukadakhala nao ulamuliro uli wonse pa Ine, ngati sukadapatsidwa kwa inu kucokera Kumwamba; cifukwa ca ici iye wondipereka Ine kwa inu ali nalo cimo loposa. (Yohane 19:10-11)

Palibe wina andicotsera uwu, koma ndiutaya Ine ndekha. Ndiri nayo mphamvu yakuutaya, ndi mphamvu ndiri nayo yakuutenganso; lamulo ili ndinalandira kwa. Atate wanga. (Yohane 10:18)

Adani a Yesu sikuti anali ndi mphanvu zopambana. Yesu anasakha kuti apereke moyo wake chifukwa cha machimo a anthu onse malingana ndi dongosolo la Mulungu. Yesu samkayenera kuchita izi. Anali ndi mphamvu zozipulumutsa Yekha pa mtanda. Mochita kufuna anaika moyo Wake pansu.

CHIUKITSO

Imfa ya Yesu pa mtanda sinali pamathero ankhani. Mphamvu ya Uthenga Wabwino simathera pano. Patapita masiku atatu chimwalireni, Yesu anauka kwa akufa. Mukhoza kuwerenga zokhudza izi mu Luka 24:1-12.

yemweyo Mulungu anamuukitsa, atamasula zowawa za imfa, mwakuti sikunali kotheka kuti iye agwidwe nayo. (Machitidwe 2:24)

Chiwonetsero chachikulu cha mphamvu ya Mulungu chinali chiukitso cha Yesu Kristu.

pakuti anapacikidwa m'ufoko, koma ali ndi moyo mu mphamvu ya Mulungu. Pakuti ifenso tiri ofok a mwa iye, koma tidzakhala ndi moyo pamodzi ndi iye, mu mphamvu ya Mulungu, ya kwa inu. (2 Akorinto 13:4)

Kuuka kwa Yesu ndi mbali yofunika kwambiri ya Uthenga Wabwino chifukwa ndi...

Koma amene mumkhululukira kanthu, inenso nditero naye; pakuti cimene ndakhululukira inenso, ngati ndakhululukira kanthu, ndacicita cifukwa ca inu, pamasopa Kristu; Pakuti ife ndife pfungo labwino la Kristu, kwa Mulungu, mwa iwo akupulumutsidwa, ndi mwa iwo akuonongeka; kwa ena pfungo la imfa kuimfa; (2 Akorinto 2:10, 15)

Kupyolera mu kuuka Kwake, Yesu anagonjetsa mphamvu ya mdani. Chifukwa chaichi, tiri ndi mphamvu pamwamba pa mphamvu ya mdani. Tiri ndi mpamvu ngakhale pa imfa, chifukwa

matupi anthuwa azalawaso chiukitso. Muli mphamvu ya ikulu muchiukitso. Paulo anayakhula zomudziwa Yesu mumphamvu yachiukitso (Afilipi 3:10). Muphonzira zambiri zokhudzana ndondomeko imeneyi mu chaputala 16, “Mphamvu ya Chiukitso Chake”

NDIPOFUNIKA CHIKHULUPIRIRO

Pali chinthu chofunika kwambiri kuti mukumane ndi cholowa cha mphamvu ya Mwazi wa Yesu Kristu. Mukuyenera kukhala ndichikulupiriro mu mwazi:

ndipo ayasedwa olungama kwaulere, ndi cisomo cace, mwa ciombolo ca mwa Kristu Yesu; kuti aonetse cilungamo cace m'nyengo yatsopano; kuti iye akhale wolungama, ndi wakumuyesa wolungama iye amene akhulupirira Yesu, Pakuti timuyesa munthu wohmgama cifukwa ca cikhulupiriro, wopanda nchito za lamulo. (Aroma 3:24-26, 28)

Ndizosakwanira kuti muli mphamvu mu Uthenga Wabwino. Mukuyenera kuyamba kugwiritsa ntchito mphamvu imeneyo mmoyo wanu. Mungachite izi kudzera muchikhulupiriro. Mukuyenera kukhulupirira mu mphamvu ya Uthenga Wabwino kuti mukumane nayo mphamvuyi. Muphonzira zambiri zokhudza ubale wa chikhulupiriro ndi mphamvu mtsogolomu mu phunziro lino.

KUKUMANA NDI MPHAMVU YA UTHENGA WABWINO

Ngati simunalandire Yesu Kristu kukhala mpulumutsi wanu ndi kukhululukidwa machimo anu, simungakumane ndi mphamvu ya Uthenga Wabwino. Kutu mukumane ndi mphamvu ya Uthenga Wabwino mukuyenera:

1. KUMVOMEREZA KUTI MUNACHIMWA:

pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu; (Aroma 3:23)

2. KUKHULUPIRIRA KUTI YESU ANAFERA MACHIMO ANU:

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. Pakuti Mulungu sanatuma Mwana wace ku dziko lapansi, kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumutsidwe ndi iye. Yohane 3:16-17

3. KUMVOMEREZA MACHIMO ANU KWA MULUNGU NDIKUMUPEPHA KUTI AKUKHULULUKIRENI:

Tikati kuti tiribe ucimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi. Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutasambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. (1 Yohane 1:8-9)

4. KUMAKHALA MOYO WOSITHIKA:

Mulore kuti mphamvu ya Uthenga Wabwino igwire ntchito mwa inu isithe makhalidwe anu akale, makhalidwe anu amachimo, ndi maganizidwe:

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Perekani tanthauzo la mau oti “Uthenga Wabwino.”

3. Kodi ndi malemba ati omwe akukamba bwino mwachidule masiko eni eni a Uthenga Wabwino?

4. Nchifukwa chiyani Uthenga Wabwino uli wa mphamvu kwambiri?

5. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira zokhudzana ndi mphamvu yomwe iri mu mwazi wa Yesu.

6. Kodi chofunika bwanji kuti mutenge mphamvu ya Uthenga Wabwino?

7. Kodi mungakumane nayo bwanji mphamvu ya Uthenga Wabwino?

8. Kodi kunena uku ndi kowona kapena kwa bodza?” Adani a Yesu anali ndi mphamvu zambiri kuposera momwe Iye anachitira chifukwa anatha kumupha Iye.” Kunena uku ndi_____.

(Mayankho amayesowa aperekedwa kumapeto bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Pitirizanibe kuphunzira za Uthenga Wabwino. Lembani mwachudule zomwe malemba otsatirawa amaphunzitsa:

Mateyu 4:23; 9:35; 24:14

Marko 1:14

Machitidwe 20:24

Aroma 1:1-3, 9; 15:16, 19

2 Akorinto 4:4

Aefeso 1:13; 6:15

1 Atesalonika 2:2, 9

1 Atesalonika 1:

2 Timoteo 1:11

1 Petro 4:17

Chibvumbulutso 14:6

CHAPUTALA 8

NDONDOMEKO YA MPHAMVU 2: MPHAMVU YA MZIMU WOYERA

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziro lino mukuyenera kukwanits zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osawonera.
- Kupereka umboni wa mmalemba omwe umawonetsera gwirizano pakati pa Mzimu Woyera ndi Mphamvu.
- Kuwonetsa cholinga chenicheni cha mphamvu ya Mzimu Woyera.
- Kufotokoza mphatso za Mzimu Woyera.
- Kulemba mndandanda kuchokera mmalemba mmene tingalandirire ubatizo wa Mzimu Woyera.

VESI YOTSOGOLERA:

Ndipo onani, Ine nditumiza pa inu lonjezano la Atate wanga; koma khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yochokera kumwamba.(Luka 24: 49)

MAU WOYAMBA

Yesu anapereka lonjezo lofunika kwambiri kwa ophunzira Ake pazokhudzana ndi mphamvu ya Uzimu:

**Ndipo onani, Ine nditumiza pa inu lonjezano la Atate wanga; koma khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yocokera Kumwamba.
(Luka 24:49)**

Mphamvu ya Uthenga Wabwino ndi mphamvu ya Mzimu Woyera. pali mfundo ziwiri zofunika pakumvetsa ndondomeko ya Baibulo pokhudzana ndi mphamvu. Mwaphunzira kale zokhudzana ndi mphamvu ya Uthenga Wabwino. Koma palinso chofunika kwambiri kuti mulandire mphamvu imeneyi ya Uzimuyi. Ndi mphamvu ya Mzimu Woyera imene inalonjezedwa ndi Yesu. Chaputala chino chifotokoza ndondomeko yofunikayi. Chaputala chino ndichiyambi chabe chazokhudzana ndi Mzimu Woyera. Kuti mphunzire mutu mozama, pezani phunziro la The Harvestime Internation Institute lotchulidwa, ”*Utumiki Wa Mzimu Woyera.*”

LONJEZANO LA MPHAMVU

Yesu anawauza otsatira Ake aza...

Yesu ananena kwa iye, Muka, kamuitane mwamuna wako, nudze kuno. Mkazi anayankha nati kwa iye, Ndiribe mwamuna. Yesu ananena naye, Wanena bwino, kuti mwamuna ndiribe; (Yohane 4:16-17)

Mzimu omwe Yesu amauyakhula ndi munthu wachitatu mu Utatu Woyera wa Mulungu, Mzimu Woyera. “anadzadza” kapena “kuvala” Ophunzira ndi mphamvu Yake.

onani, Ine nditumiza pa inu lonjezano la Atate wanga; koma khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yocokera Kumwamba. (Luka 24:49)

NGWIRIZANO WA MZIMU WOYERA NDI MPHAMVU

Zindikirani kuti mphamvu imeneyi ya uzimuyi imayenera kukhalapo potsatira kulandira Mzimu Woyera:

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko. (Machitidwe 1:8)

Mphamvu ndi Mzimu:

Pakuti Mulungu sanatipatsa mzimu wa mantha; komatu wa mphamvu ndi cikondi ndi cidziletso. (2 Timoteo 1:7)

Ndipo Yesu anabwera ndi mphamvu ya Mzimu ku Galileya; ndipo mbiri yace ya iye inabuka ku dziko lonse loyandikira. (Luka 4:14)

“Mzimu wa mphamvu” ndi Mzimu Woyera:

za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Machitidwe 10:38)

ZOLINGA ZA MPHAMVU

Mzimu Woyera amatumikira mopambana munjira zambiri miyoyo ya okhulupirira. Mzimu Woyera:

Amakhala mwa iye: (1 Akorinto 6:19) ndife kachisi kapene mmalo okhalamo Mzimu Woyera.

Umalumikizitsa anthu mu mzimu umodzi ndi Mulungu ndi okhulupirira ena: (1 Akorinto 6:17). Muli mphamvu yaikulu mungwirizano monga momwe imawonetsera nkhani yokhudzana ndi nsanja ya Babulo (onani Genesis 11; makaka vesi 6).

Amatipembedzera: (Aroma 8:26) Opembedza wa mphamvu amatipepherera ife malingana ndi chifuniro cha Mulungu.

Amapereka chitsogozo: (Yohane 16:13) Mzimu Woyera umatipangitsa ife kuti tiyende mu mphamvu osati muchisokonezo. Amatitsogorera ife kumalo a mphamvu, kuchifuniro choonadi cha Mulungu.

Amapereka chikondi cha Kristu kupyolera mwa iye: (Aroma 5:5) Muphunzira zambiri zokhudza chikondi mu chaputala chotsatira.

Amawonetsera choonadi cha Baibulo kwa iye: (2 Akorinto 2:10) Bvumbulutso la umzimu la mphamvu limabwera kupyolera mwa Mzimu Woyera.

Amatothoza: (Machitidwe 9:31 ndi Yohane 14:17, 26) Amatithoza ife munthawi yachisoni.

Amapanga anthu kukhala chifaniziro cha Kristu: (2 Akorinto 3:18) Tiribe mphamvu zosisithira tokha kuchifaniziro cha Kristu. Kufuna kuzisitha tokha ndi kukonzera kupita kuchiwonongeko. Koma kupyolera mu mphamvu ya Mzimu Woyera, tikhoza kutengera chifanizo cha Yesu.

Amatiphunzitsa: (Yohane 14:26) Phunzitsi wamkhulu amakhala mwa ife pamene tadzadziwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera. Kuzindikira ndi kofunika kwambiri, ndipo Mzimu Woyera amatigawirako chidziwitso cha Uzimu.

Unamudzutsa iye: (Aroma 8:11) Mphamvu yomweyo imene inamudzutsa Yesu kwa akumfa ikugwirabe ntchito mwa ife kuti azatidzutse. Zomwe zikutanthauza kuti tidzadzidwa matupi anthu adzadzidwa ndi mphamvu yachiukitso.

Amayeretsa: (2 Atesolanika 2:13-14) Tisamayesere kukhala moyo wachiyero patokha. Mphamvu ya Mzimu Woyera imayeretsa malingaliro anthu ndi zochita zanthu. Amabweretsa moyo wachiyero.

Amasitha iye: (Tito 3:5) Mphamvu ndiyofunika chifukwa imabweretsa kusitha nde Mzimu Woyera amapereka mphamvu yakakusitha munjira yabwino.

Amamutsutsa pa choipa: (Yohane 16:8-11) Muphonzira mtsogolomu mu phunziro lino kuti tchimo limabweretsa kulephera kwa mphamvu ya Uzimu. Mzimu Woyera umatsutsa kuchoipa ndipo umatitsogoza ife kukulapa. Izi zimapangitsa kuti mphamvu ya Mulungu iziyendabe mwa ife.

Amapereka chitsimikizo chachipulumutso: (Aroma 8:16) Kuzindikira malo anu kumakupatsani inu mphamvu. Mzimu Woyera umakupatsani inu chitsimikiza mwa Mulungu.

Amapereka ufulu: (Aroma 8:2) Ufulu umapereka mwayi waukulu okhala ndi mphamvu. Mzimu Woyera umapereka ufulu kupyolera mwa Yesu Kristu.

Amayakhula kupyolera mwa iye: (Marko 13:11) Sitikhala ndi malire chifukwa kuthekera koyakhula kwathu. Mzimu Woyera umayakhula mau a Mulungu a mphamvu ndi ulamuliro amwa ife.

Amawonetsera mphamvu ya Mulungu: (1 Akorinto 2:4) Mzimu Woyera umapanga kuthekera kowonetsera mphamvu ya Mulungu mbali zonse za moyo wanthu.

Amalimbikkitsa: (Aefeso 3:16) Pamene mwa fooka, mphamvu ya Mulungu imawonekera.

CHOLINGA CHACHIKULU

Zonsezi ndi zolinga zofunika, koma pali cholinga chachikulu cha mphamvu ya Mzimu Woyera. Zolinga zonse za Mzimu Woyera ziri ndi cholinga chofuna kukafikira cholinga chimenechi. Cholinga chachikulu cha Mzimu Woyera chinawonetseredwa mulonjezano lomwe analonjeza Yesu:

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko. (Machitidwe 1:8)

Mphamvu yokhala mboni ya Yesu ndi chizindikiro cheni cheni cha Mzimu Woyera. Asanabwere Mzimu Woyera, Petro mopanda manyazi anakana kuti samudziwa Yesu. Kutsatira kudzadzidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera, Petro anayima ndikupereka umboni wa mphamvu wa Uthenga Wabwino umene unapangitsa kuti anthu okwana zikwi zitatu apulumuke.

Inali mphamvu ya Mulungu yomwe inapangitsa mpingo woyamba kuti ufalitse Uthenga Wabwino pa dziko lonse. Buku la Machitidwe linalimba za umboni waza mphamvu Zake ndi mmene munthu angabatizidwire ndi Mzimu Woyera.

UBATIZO WA MZIMU WOYERA

Kudzadzidwa ndi mphamvu kumabwera kudzera munjira imene imatchedwa kuti”Ubatizo wa Mzimu Woyera.”

pakuti Yohane anabatizadi ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera, asanapite masiku ambiri. (Machitidwe 1:5)

Petro anayakhulapo za ubatizowu:

Ndipo ndinakumbuka mau a Ambuye, kuti ananena, Yohanetu anabatiza ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera. (Machitidwe 11:16)

CHIZINDIKIRO CHOWONEKA NDI MASO

Umboni weni weni wa ubatizo wa Mzimu Woyera ndi mphamvu ya Uzimu, koma chimenechi chimatsatana ndi chizindikiro chowoneka ndi maso. Pali malo atatu mu Chipangano Chatsopano momwe timauzidwa zomwe zinachitika pamene anthu anabatizidwa ndi Mzimu Woyera. Izi mkuphatikizaponso kuperekedwa koyamba kwa Mzimu Woyera zomwe zinalembedwa pa Machitidwe 2:2-4; mnyumba ya Koneriyo mu Machitidwe 10:44-45; ndi pamene otembenuka mtima ku Aefeso analandira Mzimu Woyera zinalembedwa mu Machitidwe 19:6.

Pofananitsa ndime zonsezi, chizindikiro chimodzi chowoneka ndi maso pali chofanana pa ndime zitatuzi. Onse amene analandira Mzimu Woyera anayakhula ndi zilakhulo zina pambali paziyakhulo zao. Ziyakhulo zimenezi sikuti anachita kuphunzira. Zinali zilakhulo zomwe analandira kupyolera mu mphamvu ya Mzimu Woyera. “Malirime” a Mzimu Woyera akhoza kukhala chiyakhulo chenicheni chomwe chimagwiritsidwa ntchito pano padziko lapansi.

Ndipo anadabwa onse, nazizwa, nanena, Taonani, awa onse alankhulawa sali Agalileya kodi? ndipo nanga ife timva bwanji, yense m'cilankhulidwe cathu cimene tinabadwa naco? (Machitidwe 2:7-8)

Malilime akhozaso kukhala chiyakhulo chosadziwika ndi munthu wina aliyense. Amenewa amatchulidwa kuti “Malirime osadziwika.”

Pakuti iye wakulankhula lilime salankhula ndi anthu, koma ndi Mulungu; pakuti palibe munthu akumva; koma mumzimu alankhula zinsinsi. (1 Akorinto 14:2)

ZOLINGA ZAMALILIME

Malirime operekedwa ndi Mzimu Woyera alindi zolinga zamphamvu miyoyo ya okhulupirira. Mwazina za zolinga za malire zomwe zikupezeka pa 1 Akorinto 14 ndi:

- **Kuyakhulana ndi Mulungu:** vesi 2
- **Kudzimangirira wekha** : Kuzimangirira sikuzikweza wekha, koma zikutanthauza kuti kuzilimbikitsa, kusintha, ndikuzitukula. Vesi 4
- **Akamasuliridwa, amamangirira Mpingo:** vesi 12
- **Kupembedzera:** vesi 14. Onaniso Aroma 8:26-27
- **Matamando:** Vesi 15,17
- **Kukwaniritsidwa kwa uneneri:** Vesi 21. Onaniso Yesaya 28:11-12
- **Chizindikiro kwa osakhulupirira:** Vesi 22. Onaniso Machitidwe 2

MPHATSO ZA MZIMU WOYERA

Yesu anawasiyira ophunzira ake ulamuliro ofalitsa Uthenga Wabwino kufikira kumalekezera a dziko lapansi:

Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansu pano. (Mateyu 28:19-20)

Mphamvu ya Mzimu Woyera inaperekedwa kuti ithandize okhulupirira kukwaniritsa ntchito imeneyi (Machitidwe 1:8).

Mbali ina ya mphamvu ya Mzimu Woyera ndi mphatso za uzimu zomwe Mzimu Woyera amapereka kwa okhulupirira kuti ziwakozekeretse kukatumikira mwamphamvu. Ntchitoyi ndiyaikulu sngakwaniritsidwe ndikuthekera kwakunthupi.

Mphatso za uzimu sizofanana ndi luso lobadwa nalo. Mphatso ndi luso lakuthupi zimaperekedwa pobadwa kudziko lapansi kapena zimabwera chifukwa chakulimbikira kwa munthu. Koma zikhoza kugwiritsidwaso ntchito mu utumiki, koma izi chimodzi modzi ngati mphatso za Uzimu.

Mphatso za Uzimu ndi kuthekera kwa mphamvu kopatsidwa ndi Mzimu Woyera ndi cholinga chokakwanitsa utumiki. Mphatso za Mzimu Woyera ndi kuthekera koperekedwa ndi Mulungu...

kuti akonzere oyer mtima: ku nchito ya utumiki, kumangirira thupi la Kristu; kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa cikhulupiriro, ndi wa cizindikiritso ca Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa cidzaloca Kristu. Kuti tisakhaleenso makanda, ogwedezekagwedezeka, natengeka-tengeka ndi mphepo yonse ya ciphunzitsa, ndi tsenga la anthu, ndi kucenjerera kukatsata cinyengo ca kusoceretsa; koma ndi kucita zoonna mwa cikondi tikakule m'zinthu zonse, kufikira iye amene ali mutu ndiye Kristu; (Aefeso 4:12-15)

Ndime yayikulu imene yapereka ndandanda wa mphatso za uzimu kwa okhulupirira kupyolera kwa Mzimu Woyera ndi: Aroma 12:1-8; 1 Akorinto 12:1-31; Eafeso 4:1-16; 1 Petro 4:7-11.

Nawo ndandanda wa mphatso za uzimu. (Baibulo silinapereke mndandanda malingana ndi magulu amene aperekedwa pano. Magulu awa aperekedwa chifukwa chofuna kuphunzira.)

Mphatso zapaderadera

Atumwi

Aneneri

Alaliki

Abusa

Aphunzitsi

Mphatso zotumikira

Kuzindikira mizimu

Utsogoleri

Kuyendetsa zinthu

Kupereka

Kuthandiza

Kutumikira

Mphatso zoyakhula

Uneneri

Kuphunzitsa

Kulimbikitsa

Mau anzeru

Mau achidziwitso

Mphatso zazizindikiro

Zozizwa

Kuchilitsa

Malirime

Sukulu ya Harvestime International iri ndi phunziro, “*Utumiki wa Mzimu Woyera,*” lomwe limafotokoza bwino mphatso iriyonse mwatsatanetsatane. Izakuthandizani kuti muzindikire mphatso yanu ya uzimu mmoyo mwanu. Makhalidwe amenewa matchulidwa kuti chipatso cha Mzimu. Chipatso cha Mzimu ndi chikhalidwe cha Mzimu Woyera chomwe chimawonekera mmoyo wa wokhulupirira. Mulungu amafuna kuti chipatso chimenechi chiwonekere mmoyo mwanu. Ndiye uwu ndi ndandanda wa chipatso cha Mzimu Woyera.

Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, icikhulupirtro, cifatso, ciletso; pokana zimenezi palibe lamulo. Koma iwo a Kristu Yesu adapacika thupi, ndi zokhumba zace, ndi zilakolako zace. (Agalatiya 5:22-23)

Chipatso cha Mzimu Woyera chafotokozedwa bwino mu phunziro lotchedwa, “*Utumiki wa Mzimu Woyera.*” Chikhalidwe chimenechi chimakupatsani mphamvu ya uzimu yofanana ndi Yesu.

KULANDIRA KUDZADZIDWA NDI MPHAMVU

Monga mmene Yesu analonjezera, Mzimu Woyera unaperekedwa ndi Atate mmene ophuzira amakadikirira ku Yerusalemu (Machitidwe 2). Mzimu Woyera unaperekedwa kale, koma okhulupirira aliyense akuyenera kulandira mphamvu imeneyi pakudzera mu ubatizo wa Mzimu Woyera..

Izi ndi njira za m’Baibulo kuti mulandire ubatizo wa Mzimu Woyera:

LAPANI NDIPO BATIZIDWANI:

Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. (Macitidwe 2:38)

KHULUPIRIRANI KUTI NDI ZA INU:

Pakuti lonjezano 1 liri kwa inu, ndi kwa ana anu, 2 ndi kwa onse akutali, 3 onse amene Ambuye Mulunguwathu adzaitana... (Macitidwe 2:39)

MUFUNITSITSE (KUFUNITSITSA):

Koma tsiku lomariza, lalukurulo la phwando, Yesu anaimirira napfuula, ndi kunena, Ngati pali munthu akumva Ludzu, adze kwa Ine, namwe. Iye wokhulupirira Ine, monga cilembo cinati, Mitsinje ya madzi amoyo idzayenda, kuturuka m'kati mwace. Koma 1 ici anati za Mzimu, amene iwo akukhulupirira iye anati adzalandire; pakuti Mzimu panalibe pamenepo, cifukwa Yesu sanalemekezedwa panthawi pomwepo. (Yohane 7:37-39)

MUMUVOMEREZE NGATI MPHATSO:

Mzimu Woyera anaperekedwa kale. Anaperekedwa ku mpingo pa tsiku la pentekosite. Chifukwa chakuti iye ndi mphatso, simungachite kalikonse kuti mumulandire:

Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Macitidwe 2:38

ici cokha ndifuna kuphunzira kwa inu, Kodi munalandira Mzimuyo ndi nchito za lamulo, kapena ndi kumva kwa cikhulupiriro? Ndipo iye amene akuonjezerani inu Mzimuyo, nacita zimphamvu mwa inu, atero kodi ndi nchito za lamulo, kapena ndi kumva kwa cikhulupiriro? kutidalitso la Abrahamu mwa Yesu Kristu, licitike kwa amitundu; kuti tikalandire lonjezano la Mzimuyo, mwa cikhulupiriro. (Agalatiya 3:2,5,14)

Yambani kukweza ndi kuyamika Mulungu chifukwa cha mphatso ya Mzimu Woyera.

DZIPEREKENI KWA MULUNGU:

Perekani lilime lanu kwa Mulungu pakumkwekweza ndi kupembedza Mulungu. Pamene mukukweza Mulungu mokweza mawu mutha kuyamba kumva ngati chibwibwi m' milomo yanu. Pamene mukupitiriza kupereka lilime lanu kwa Mzimu Woyera iye adzayamba kuyankhula kudzera mwa inu m' mawu achilendo. Ichi ndi zindikiro chowoneka chotsimikiza ubatizo wa Mzimu Woyera:

Iai, koma ndi anthu a milomo yacilendo, ndi a lilume lina, Iye adzalankhula kwa anthu awa; (Yesaya 28:11)

Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa. (Macitidwe 2:4)

KUPEMPHA MAPEMPHERO A OKHULUPIRIRA ENA:

Mzimu Woyera atha kulandiridwa pakusanjikidwa manja. (Machitidwe 8,9,19) kapena opanda kusanjikidwa manja (Machitidwe 2,4,10). Werengani ma chaputala amenewa amene akuwonetsa momwe okhulupirira odzadzidwa ndi Mzimu Woyera angakuthandizireni kubatizidwa ndi Mzimu Woyera.

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Perekani umboni wa Mmalemba owonetsera gwirizano pakati pa Mzimu Woyera ndi mphamvu.

3. Kodi cholinga chachikulu cha mphamvu ya Mzimu Woyera ndi chani?

4. Perekani malemba a m’Baibulo amene ali ndi mndandand wa chipatso cha Mzimu Woyera.

5. Lembani njira zisanu ndi imodzi zomwe zaperekedwa mu chaputala chino kuti mulandire mphamvu ya Mzimu Woyera.

6. Gwiritsani ntchito ndime zotsatirazi kuti mulembe mndandanda wa mphatso za Mzimu Woyera zomwe ziri zopezeka kwa okhulupirira: Aroma 12:1-8; 1 Akorinto 12:1-31; Aefeso 4:1-16; 1 Petro 4:7-11.

(Mayankho amayesowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Werengani Machitidwe 8:14-17. Anthu aku Samariya analandira chipulumutso kupyolera mu utumiki wa Filipi. Analandira ubatizo wa Mzimu Woyera kupyolera mu utumiki wa Petro ndi Yohane.

Kulandira ubatizo wa Mzimu Woyera zinali zosiyana ndi kulandira chipulumutso. Izi zikuwonetsera mphamvu ya Uthenga Wabwino ndi mphamvu ya Mzimu Woyera kugwira ntchito limodzi muutumiki.

Onaniso Machitidwe 19:1-6. Onaniso funso la Paulo: “Kodi munalandira Mzimu Woyera pamene munakhulupirira?”

2. Pezani buku la sukulu ya Harvestime International lotchedwa “Utumiki wa Mzimu Woyera.’ Iyi ndi ndondomeko yatsatanetsane ya utumiki wa mphamvu ya Mzimu Woyera miyoyo ya okhulupirira. Chifungulo chenicheni cha mphamvu ya uzimu chimawonetsera mphatso zanu za Uzimu ndipo zimabala chipatso mmoyo mwanu. Phunziroli likuthandizani pa zimenezi.

Ngati mukutenga maphunziro a Institute mundandanda umenewu, ndekuti mwaphunzira kale “Utumiki wa Mzimu Woyera.” Onaniso kachikena ndi cholinga chopeza njira yomwe Mzimu Woyera umakozekeretsa okhulupirira ku utumiki wa mphamvu.

CHAPUTALA 9

NDONDOMEKO YA MPHAMVU 3: MPHAMVU YA CHIKONDI

ZOLINGA:

Pomaliza paphunziroli mukuyenera kukwaniritsa izi:

- Kulemba Vesi yotsogolera mosawonera.
- Kupereka tanthauzo la “chikondi.”
- Kupereka tanthauzo la “chifundo.
- Kuwonetsera chikondi ngati ndondomeko yapamwamba ya mphamvu ya uzimu.
- Kulozera lamulo loyamba ndi lachiwiri loponsa zonse.
- Kufotokoza mmene dziko lingadziwirekuti ndife okhulupirira.

VESI YOTSOGOLERA:

Ndipo tsopano zitsala chikhulupiriro, chiyembekezo, chikondi, zitatatu izi; koma chachikulu cha izi ndicho chikondi. (2 Akorinto 13:13)

MAU OYAMBA

Mu chaputala chapitachi munaphunzira zokhudzana mphamvu ya Mzimu Woyera.

Munaphunzira kuti chipatso cha Mzimu ndi chomwe chimawonetsera mphamvu yobwera ndi Mzimu Woyera mmoyo mwa okhulupirira. Chimodzi mwa zipatso ndi kukhala ndi chikondi monga mwachikhalidwe ngati Kristu. Ndi chipatso choyamba pa mndandanda wa pa Agalatiya 5:22-23:

Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, icikhulupiriro, (Agalatiya 5:22)

MPHAMVU YOPAMBANA

Werengani 1 Akorinto 13:1-13 musanapitire ndi phunziroli. Mau oti “chifundo” mundime imeneyi akutanthauza chikondi. Chaputalachi chikukhazikika kwambiri pa ndondondomeko ya mphamvu ya uzimu, mphamvu ya chikondi. Mphamvu ya chikondi imaposa iriyonse.

Malilime amaperekedwa ndi Mzimu Woyera: Tsiku lina malilime onsewa azasiya. Kaya mumayakhula malilire odziwika kapena osadziwika kwa anthu, ngati palibe chikondi muli chabe (Vesi 1 ndi 8)

Chidziwitso ndi kumvetsetsa: Chidziwitso ndi champhamvu, koma tsiku lina chidziwitso cha umunthu chizasowa. Chikondi chizakhalabe. (Vesi 2 ndi 8)

Mphatso ya uneneri: Imeneyi ndi mphatso yopambana kwambiri. Kukhala ndikuthekera kuyakhula uthenga wa Mulungu mwachindunji komaso kunenera zinthu zamtsogolo. Koma uneneri tsiku lina uzalekeka. (Vesi 2,8-12)

Chikhulupiriro: Ngakhale mutakhala ndi chikhulupiriro chosutha mapiri chiri chabe ngati mulibe chikondi. (Vesi 2)

Kupereka: Ngakhale mutapereka kwambiri kwa ena, ndizosapanda ngati mupereka opanda chikodi ndizonda pake. (Vesi 3)

Kufa chifukwa cha Uthenga Wabwino: Ngakhale mutakhala kuti mwafera Uthenga Wabwino, ndi msembe yopanda pake pokhapokha ngati mupanga zimenezi ndi chikondi. (Vesi 3)

Chiyembekezo: Chiyembekezo ndi chofunika kwambiri chifukwa kupanda ichi moyo umakhala owawa kwambiri. Koma chikondi ndi chopambana kuposa chiyembekezo. (Vesi 13)

Mwaphunzira ndipo mupitiriza kuphunzira zambiri zokhudzana mphamvu yauzimu mu phunziroli. Koma kumbukirani ichi: Ndongomeko zina zonse za mphamvu, mphatso zonse za uzimu, mautumiki onse akuyenera kugwira ntchito kudzera mu mphamvu ya chikondi, kupanda apo ndekuti zonse ziri chabe. Pamene zonse zalephera, mphamvu ya chikondi idzapambana.

TANTHAUZO NDI MAKHALIDWE A CHIKONDI

Chikondi ndi chikhalidwe chachikondi chozama, kusamalira, ndikukhudzika zomwe zimabwera mmoyo mwanu kupyolera mwa Mzimu Woyera.

ndipo ciyembekezo sicicititsa manyazi; cifukwa cikondi ca Mulungu c inatsanulidwa m'mitima mwathu mwa Mzimu Woyera, amene wapatsidwa kwa ife. (Aroma 5:5)

Dziwani kuti makhalidwe a chikondi cha umulungu aperekedwa pa 1 Akorinto 13:

VESI 4:

Chikondi chimapirira.

Chikondi ndi chokoma mtima.

Chikondi sichidzitama, sichidzikuza.

VESI 5:

Chikondi sichichita zosayenera (kuchitira ena zoipa)

Chikondi sichichita za mwini yekha (sichichikonda)

Chikondi sichipsa mtima (Sichikwiya)

Chikondi sichilingirira zoipa.

VESI 6:

Chikondi sichikondwera ndi zoipa (Sichikondwera pakuchita zoipa kapena kumva zoipa za ena)

Chikondi chimakondwera ndi chilungamo (osati ndi bodza ndi miseche)

VESI 7:

Chikondi chimakwirira zinthu zonse (ngakhale zowawitsa)

Chikondi chimayembekezera zinthu zonse (sichimataya chiyembekezo chamwa Mulungu, posayang'anira nyengo)

Chikondi chipirira zinthu zonse.

VESI 8:

Chikondi sichilephera (posayang'anira nyengo)

ZOMWE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZOKHUZANA NDI CHIKONDI

Kuti mumvetsetse mphamvu ya chikondi, mukuyenera kudziwa zomwe Baibulo limaphunzitsa pa mutu umenewu. Chipatso cha uzimu cha chikondi, mphamvu yopambanayi, si mtundu wa zogonana, kapena chikondi chakunthupi choperekedwa ndi dziko. Chikondi chimenechi “ndi chosanyenga,”kutanthauza kuti ndi chikondi choyera. Chikondi chosanyenga ndi chikondi chimene mukuyenera kuwonetsera kwa ena:

Popeza 5 mwayeretsa moyo wanu pakumvera coonadi kuti 6 mukakonde abale ndi cikondi cosanyenga, mukondane kweni kweni kucokera kumtima; (1 Petro 1:22

Lamulo lalikulu loyamba ndi lakuti mukuyenera kukonda Mulungu:

ndipouzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mphamvu yako yonse. (Marko 12:30)

(Onaniso Deuteronome 6:5; Luka 10:27; 1 Yohane 2:5;15; 3:11-17;4:7-20; 5:2; 2 Yohane 1:5-6)

Chikondi chanu pa Mulungu chimayesedwa pakumvera kwanu kwa Iye:

Yesu anayankha nati kwa iye, Ngati wina akonda Ine, adzasunga mau anga; ndipo Atate wanga adzamkonda, ndipo tidzadza kwa iye, ndipo tidzayesa kwa iye mokhalamo. (Yohane 14:23)

koma iye amene akasunga mau ace, mwa iyeyu zedi cikondi ca Mulungu cathedwa. M'menemo tizindikira kuti tiri mwa iye; (1 Yohane 2:5)

Lamulo lachiwiri lalikulu ndi chikondi cha pa ena:

Laciwiri ndi ili, Uzikonda mnzako monga udzikonda mwini. Palibe lamulo lina lakuposa awa. (Marko 12:31)

Yesu akufuna kuti inu muzikondaso ena monga momwe Iye amakukonderani inu:

Ndikupatsani inu lamulo latsopano, kuti mukondane wina ndi mnzace; monga ndakonda Inu, kuti inunso mukondane wina ndi mnzace. (Yohane 13:34)

Monga momwe Atate wandikonda Ine, Inenso ndakonda inu; khalani m'cikondi canga. Lamulo langa ndi ili, kuti mukondane wina ndi mnzace, monga ndakonda inu. (Yohane 15:9, 12)

Yohane 17:26

Ndi kupyolera muchikondi zomwe zimakuzindikiritsani kuti ndinu wokhulupirira:

ndinazindikiritsa iwo dzina lanu, ndipo ndidzalizindikiritsa; kuti cikondi 7 cimene munandikonda naco cikhale mwa iwo, ndi Ine mwa iwo. (Yohane 13:35)

Ife tidziwa kuti tacokera kuturuka muimfa kulowa m'moyo, cifukwa tikondana ndi abale iye amene sakonda akhala muimfa. (1 Yohane 3:14)

Ngati simumakonda okhulupirira ena, chikondi cha Mulungu sichiri mwa inu:

itye amene anena kuti ali m'kuunika, namuda mbale wace, ali mumdima kufikira tsopane lino. Iye amene akonda mbale wace akhala m'kuunika, ndipo mwa iye mulibe cokhumudwitsa. (1 Yohane 2:9-10)

(Ichi ndi chowonadi chofunika. Pitirizani kuphunzira Yohane 13:34; 14:15, 21, 23,31; 15:9-17; 17:26; 21:15-17)

Chikondi chokonda okhulupirira ena chimabwera chifukwa cha ngwirizano wa uzimu umene ndi wamphamvu kwambiri. Pamene anali mu umodzi mu pephero, Pentekosti anachitika (Machitidwe 2). Anali ndi “mtima ndi maganizo amodzi” ndipo ndi mphamvu anapitirirabe kuchitira umboni (Machitidwe 4:32-33). Anadzipereka okha kungwirizano wa chiyanjano ndipo zozizwa ndi zizindikiro zambiri zinachitika (Machitidwe 2:42-43)

Mukuyenera kukonda adani anu:

Koma ndinena kwa inu akumva, Kondanani nao adani anu; citirani zabwino iwo akuda inu, dalitsani iwo akutemberera inu, pemphererani iwo akucitira inu cipongwe. Ndipo ngati muwacitira zabwino iwo amene akucitirani, inu zabwino, mudzalandira ciyamiko cotani? pakuti anthu ocimwa omwe amacita comweco. Koma 3 takondanani nao adani anu, ndi kuwacitira zabwino, ndipo kongoletsani osayembekeza kanthu konse, ndipo mphotho yanu idzakhala yaikuru, ndipo 4 inu mudzakhala ana a Wamkurukuruyo; cifukwa iye acitira zokoma anthu osayamika ndi oipa. (Luka 6:27, 28, 33, 35)

Munamva kuti kunanenedwa, 14 Uzikondana ndi mnansi wako, ndi kumuda mdani wako: koma Ine ndinena kwa inu, 15 Kondanani nao adani anu, ndi 16 kupempherera iwo akuzunza inu; (Mateyu 5:43-44)

Chikondi chanu chikuyenera kusefukira, zomwe zikutanthauza kuti chikuyenera kupitirira kumakulabe:

(Afilipi 1:9)

koma Ambuye akukulitseni inu, nakueurukitseni m'cikondano wina kwa mnzace ndi kwa anthu onse, monganso ife titero kwa inu; (1 Atesalonika 3:12)

Mukuyenera kumera ndikukhazikika mu chikondi:

kuti Kristu akhale cikhaliro mwa cikhulupiriro m'mitima yanu; kuti, ozika mizu ndi otsendereka m'cikondi, mukakhozetu kuzindikira pamodzi ndi oyera mtima onse, kupingasa, ndi utali, ndi kukwera, ndi kuzama nciani; ndi kuzindikira cikondi ca Kristu, cakuposa mazindikiridwe, kuti mukadzazidwe kufikira cidzalo conse ca Mulungu. (Aefeso 3:17-19)

Ngati mukufuna kuti mudzadzidwe ndi umphumphu wa Mulungu ndi mphamvu Yake, mukuyenera kukhala ndi chikondi, izi ndi zofunika ku mphamvu chifukwa chimachotsa mantha.

Mulibe mantha m'cikondi; koma cikondi cangwiro citaya kunja mantha, popeza mantha ali naco cilango, ndipo wamanthayo sakhala wangwiro m'cikondi. (1 Yohane 4:18)

Mukuyenera kuyenda muchikondi:

ndi kuonetsera kudzicepetsa konse, ndi cifatso, ndi kuonetsera cipiriro, ndi kulolerana wina ndi mnzace, mwa cikondi; (Aefeso 4:2)

Mukuyenera kuyanjana ndi ena mchikondi:

ndi kuonetsera kudzicepetsa konse, ndi cifatso, ndi kuonetsera cipiriro, ndi kulolerana wina ndi mnzace, mwa cikondi; (Aefeso 4:2)

Mukuyenera kuzisunga nokha mchikondi:

mudzisunge nokha m'cikondi ca Mulungu, ndi 5 kulindira cifundo ca Ambuye wathu Yesu Kristu, kufikira moyo wosatha. (Yuda 21)

Koma iwe, munthu wa Mulungu iwe, thawa izi; nutsate cilungamo, cipembedzo, cikhulupiriro, cikondi, cipiriro, cifatso. (1 Timoteo 6:11)

Chikhulupiriro, chomwe chili chofunika kwambiri, chimagwira ntchito ndi chikondi:

Pakuti mwa Kristu Yesu kapena mdulidwe kapena kusadulidwa kulibe mphamvu; komatu cikhulupiriro cakucititsa mwa cikondi. (Agalatiya 5:6)

Ntchito yanu kwa Ambuye ikuyenera kugwiridwa ndi chikondi:

Ndi kukumbukila kosalekeza nchito yanu ya cikhulupiriro, ndi cikondi cocitacita, ndi cipiriro ca ciyembekezo ca Ambuye wathu Yesu Kristu, pamaso pa Mulungu Atate wathu; (1 Atesalonika 1:3)

pakuti Mulungu sali wosalungama kuti adzaiwala nchito yanu, ndi cikondico mudacionetsera ku dzina lace, umo mudatumikira oyera mtima ndi kuwatumikirabe. (Ahebri 6:10)

Pamene tikuyandikira kuchimaliziro cha dziko lapansi, chikondi cha anthu ambiri chidzazirala. Chizazirala kutanthauza kuti anthu azakhala osasamala za ena:

Ndipo cifukwa ca kucuruka kwa kusayeruzika, cikondano ca anthu aunyinji cidzazirala. (Mateyu 24:12)

Koma tapatsidwa chitsimikizo kuti palibe chimene chizatirekanitse ife ndi chikondi cha Mulungu:

Adzatisiyanitsa ndani ndi cikondi ca Kristu? nsautso kodi, kapena kupsinjika mtima, kapena kuzunza, kapena njala, kapena usiwa, kapena zoopsya kapena lupanga kodi? (Aroma 8:35, 38-39)

YESERO LALIKU LA CHIKONDI

Chikondi chachikulu ndi chikondi chimene Mulungu alinacho pa ochimwa. Anawonetsera chikondi chimenecho potumiza Yesu kuzafa:

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. (Yohane 3:16)

Yesu anawonetsera chikondi chopambanachi pamene anaperaka moyo Wake pa mtanda:

Palibe munthu ali naco cikondi coposa ici, cakuti munthu ataya moyo wace cifukwa ca abwenzi ace. (Yohane 15:13)

Pakuti ndi cibvuto munthu adzafera wina wolungama; pakuti kapena wina adzalimbika mtima kufera munthu wabwino. Koma g Mulungu atsimikiza kwa ife cikonai cace ca mwini yekha m'menemo, kuti pokhala ife cikhaliwe ocimwa, Kristu adatifera ife. (Aroma 5:7-8)

Ndi mphamvu yaikulu ya chikondi chikondi cha Mulungu chimene Mzimu Woyera akufunitsitsa kuti aikize mmoyo mwanu:

ndipo ciyembekezo sicicititsa manyazi; cifukwa cikondi ca Mulungu cinatsanulidwa m'mitima mwathu mwa Mzimu Woyera, amene wapatsidwa kwa ife. (Aroma 5:5)

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi yotsogolera osawonera.

2. Kodi chikondi chiani?

3. Kodi lamulo lalikulu loyamba ndi lachiwiri ndi liti?

4. Kodi dziko lingadziwe bwanji kuti ndife okhulupirira?

5. Malizitsani ndime iyi:

“Ndondomeko zina zonse za mphamvu ya uzimu, mphatso zonse za uzimu, ma utumiki onse akuyenera kugwira ntchito kupyolera mu mphamvu ya _____ kupanda apo ndekuti ali opanda pake.”

6. Kodi ndondomeko yopambana ya mphamvu ya uzimu ndi chani?

(Mayankho amayesowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Davide analemba zambiri zokhudzana ndi chikondi. Onani Masalimo 18:1; 31:23; 40:16; 97:10; 116:1; 119:97, 113, 119, 127, 132, 159, 163, 165, 167; 122:6; 145:20.
2. Werengani book la 1 Yohane. Chiphunzitso chachikulu chabukuli ndi chikondi.
3. Iyi ndi 1 Akorinto 13 mumamasuliridwe a Baibulo okweza omwe akupereka kuwonjezera kwa tanthauzo la liu la chikondi mu mmalemba:

Ngati ndi ngalakhule ndi malirime a anthu ngakhale a Angelo, koma ngati ndilibe chikondi ndili ngati belu la mpokoso.

Ndipo ngati ndili ndi mphamvu ya uneneri nde mphatso ya kumasulira chifunilo ndi cholinga chakumwamba; ndikumvetsa zisisi zenizeni ndikukhala ndi chidziwitso chonse, ndipo ngati ndili ndi chikhulupiriro chachikulu chosuntha mapiri, koma ngati ndiribe chikondi ndiri chabe.

Ndingakhale ndipereka zonse zomwe ndiri nazo (popereka kwa osauka) chakudya, ndipo ngakhale ndipereka thupi langa litethedwe moto koma ngati ndiribe chikondi (chikondi cha Mulunu mwa ine), sindipindula kanthu.

Chikondi ndi choreza, chiri chokoma mtima; chikondi sichidukidwa; chikondi sichiziwa kuzitamandira, sizichikuza, sichichita zosayenera, sichitsata za mwini yekha, sichipsa mtima.

Sichichita zosayenera, sichita mwano, chikondwera ndi chinyengo, chikondi chikhala choreza. Pakuti ife tidziwa mderamdera, ndimo tinena mderamdera. Koma pamene chagwirowo chafika, tsono chamderamdera chidzakhala chabe. Pamene ndinali ngati mwana, ndinalakhula ngati mwana, ndinalingalira ngati mwana, ndinawerenga ngati mwana, ndinawerenga ngati mwana; tsopano ndakhala munthu, ndayesa chabe zachibwana. Pakuti tsopano tipenya m'kalirole, ngati chimbudzi; koma pomwepo mason di maso. Tsopano ndizindikira mderamdera; koma pomwepo ndizazindikiratu, monganso ndazindikira. Ndipo tsopano zitsala chikhulupiriro, chiyembekezo, chikondi, zitatu izi; koma chachikulu cha izi ndicho chikondi.

CHAPUTALA 10

NDONDOMEKO YA MPHAMVU 4:

KUDZODZA KWA MPHAMVU

ZOLINGA:

Polimaliza phunziriro mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osawonera.
- Kufotokoza cholinga chakudzodza kupotulika mu Chipangano Chakale.
- Kupereka zitsanzo momwe kudzodza kopatulika kumkagwiritsiridwira ntchito mu Chipangano Chakale.
- Kupereka tanthauzo la dzina loti “Kristu.”
- Kulemba mwachidule zolinga za kudzodza kwa mphamvu.
- Kufotokoza ubwino wakuzindikira kudzodza kwanu kwapaderadera mu utumiki.
- Kufotokoza mmene mungalandirire kudzodza kwa mphamvu.
- Kulozera komwe kudzodza kwa uzimu kumachokera.

VESI YOTSOGOLERA:

Ndipo inu, kudzodza munalandira kuchokera kwa Iye, kukhala mwa inu, ndipo simusowa kuti wina akuphunzitseni; koma monga kudzodza kwake kukuphunzitsani za zinthu zonse, ndipo kuli koona, sikuli bodza ayi, ndipo monga kudaphunzitsa inu, mukhale mwa Iye.(1 Yohane 2:27)

MAU WOYAMBA

Chaputala ichi chikhudza kudzodza kwa Mulungu komwe kumapereka mphamvu kwa amuna ndi akazi kuti akhale ndi utimiki wopambana.

MCHITIDWE WODZODZA

“Kudzodza” kumatanthauza kuti kuthira mafuta pa munthu kapena chinthu. Ndi mchitidwe umene unakhazikidwa munthawi ya Chipangano Chakale. Kudzodza kunali magawo atatu: Mwawamba, kwamakhwala, ndi koyera.

Kudzodza kwawamba: kumkakhudzana ndi kuzisamalira kwa munthu kuti azinukhira bwino. Mukhoza kuwerenga kugwiritsidwa ntchito kake mu Rute 3:3, Salimo 104:15, ndi Miyambo 27:9. Alendo amkadzodzedwa ngati chizindikiro cha ulemu (Luka 7:46) matupi akufa amkakozedwa kuti akaikidwe (Marko 14:8; 16:1)

Kudzodza kwa mankhwala: kumkagwiritsidwa ntchito pakuthandiza odwala ndi ovulala. Mwachitsanzo, onani Luka 10:34.

Kudzodza kopatulika: Kudzodza kwa chitatu nde mutu wa phunziro wa chaputala chino. Ndikudzodza koyera kapena ka zolinga za uzimu. kumkwagwiritsidwa ntchito popereka zinthu kapena anthu kwa Mulungu.

ZITSANZO ZA M'CHIPANGANO CHAKALE

Kudzodza koyamba kwa zolinga za uzimu kunalembedwa mu Chipangano Chakale kukupezeka mu Genesis 28:18. Kutsatila pamene Yakobo anawona masophenya akulu kuchokera kwa Mulungu.

Yakobo ndipo ankauka m'mamawa, natenga mwala umene anaika pansu pa mutu wace, nauimiritsa, nathira mafuta pamtu pace. Ndipo anacha dzina la pamenepo Beteli; pakuyamba dzina lace la mudziwo ndi Luzi. (Genesis 28:18-19)

Kenako Mulungu anayakhulapo pa zazimenezi ndipo Anati:

Ine ndine Mulungu wa ku Beteli, kuja unathira mafuta pamwala paja, pamene unandilumbirira ine cilumbiriro: tsopano uka, nucoke m'dziko lino, nubwerere ku dziko la abale ako. (Genesis 31:13)

Kenako, Mulungu anapereka malangizo okhudzana ndikudzodza amsembe, mafumu, ndi aneneri kuwapatula pazolinga za uzimu. Zokhala mu Tabenako wopembedzeramo zimkayeneraso kudzodzedwa. Mukhoza kuwerenga zambiri za izi “popitiriza kuphunzira” mbali zina za chaputala chino.

Cholinga cha kudzodza anthu awa ndi zinthu kunali kuwapatula munjira yowapereka ku ntchito ya Mulungu. Mafuta Woyera amkagwiritsidwa ntchito pa zolinga zauzimuzi.

ndipo ukonze nazo mafuta odzoza opatulika, osanganizika monga mwa macitidwe a wosanganiza; akhale mafuta odzoza opatulika. Nulankhule ndi ana a Israyeli, ndi

**kuti, Awa ndi mafuta odzoza opatulika a Ine mwa mibadwo yanu.
(Eksodo 30:25, 31)**

KUDZODZEDWA KWA YESU

Ndondomeko zotsatirazi zinaperekedwa ndi Mulungu, Yesu anadzodwe kuti akagwire ntchito. Yesu anati:

Mzimu wa Ambuye uli paine, Cifukwa cace iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino: Anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru ophwanyika, Kulalikira caka cosankhika ca Ambuye. (Luka 4:18-19)

Uku kunali kukwaniritsidwa kwa uneneri umene unaperekedwa mu Yesaya 61:1.

Ophunzira a Yesu anazindikira kuti...

Za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Machitidwe 10:38)

KOCHOKERA KUDZODZA

Mphamvu zakudzodza kwa uzimu siziri mu mafuta mokha. Mphamvu sikhala mwa munthu amene akugwira ntchito yodzodzayo kapena kuthekera kwa wodzodzedwayo. Mphamvu ya kudzodza imayenda kuchokera kuchiyambi kwake, Mulungu Atate. Zindikirani kuti Yesu anati : “Mzimu wa Ambuye uli pa Ine pakuti wandidzodza Ine.”

Paulo anati:

Koma iye wakutikhazika pamodzi ndi inu kwa Kristu, natidzoza ife, ndiye Mulungu; (2 Akorinto 1:21)

Mulungu ndi amene anali kochokera kudzodza kwa Kristu ndipo anakalibe kochokera kudzodza. Mafuta ndi chizindikiro chakuthupi chabe chogwiritsidwa ntchito kuimirira kudzodza kumeneku. Yesu anagwiritsa ntchito nchitidwe odzodza, koma osati nthawi zonse ndi mafuta. Wakhungu atachiritsidwa ndi Yesu anati:

Iyeyu anayankha, Munthuyo wochedwa Yesu anakanda thope, napaka m'maso mwanga, nati kwa ine, Muka ku Siloamu kasambe; cifukwa cace ndinacoka, ndipo m'mene ndinasamba ndinapenya, (Yohane 9:11)

Vesi imeneyi ikutsimikiza kuti sizinthu zomwe zagwiritsidwa ntchito koma ndi mphamvu imene iri kumbuyo kwa kudzodzako ndi imene iri ndi mphamvu. Ngakhale amuna ndi akazi amkadzodzedwa ndi mafuta ndi anthu, mphamvu yeniyeni yakudzodza imakachokera kwa Mulungu. Mulungu anati za Davide:

Ndapeza Davide mtumiki wanga; Ndamdzoza mafuta anga oyera. (Masalimo 89:20)

Zaka zambiri asanadzodzedwe ndi munthu, Davide anali atadzodzedwa kale ndi Mulungu:

Ndipo Natani ananena kwa Davide, Munthuyo ndi inu nomwe. Atero Yehova, Mulungu wa Israyeli, Ndinakudzoza ukhale mfumu ya Israyeli, ndinakupulumutsa m'dzanja la Sauli; (2 Samueli 12:7)

ZOLINGA ZA KUDZODZA

Kudzodza kwa Mzimu wa Mulungu ndikofunika kwambiri mmoyo ndi utumiki wa wokhulupirira. Nde nazo zina za zolinga za kudzodza:

KUGWIRA NTCHITO:

Pamene kudzodza kwa Mulungu kunabwera pa Sauli, anasandulika kukhala munthu wa tsopano kuti atumikire Israeli monga mfumu:

Pamenepo Samueli anatenga nsupa ya mafuta, nawatsanulira pamutu pace, nampsona iye, nati, Sanakudzoza ndi Mulungu kodi, mukhale mfumu ya pa colowa cace? ndipo Mzimu wa Yehova udzagwera inu kolimba, nanunso mudzanenera pamodzi nao, nimudzasandulika munthu wina. (1 Samueli 10:1, 6)

Yesu anadzodzedwa ndi Mulungu kuti akagwire ntchito:

Mzimu wa Ambuye uli paine, Cifukwa cace iye anandidzoza Ine ndiuzo anthu osauka Uthenga Wabwino: Anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru ophwanyika, Kulalikira caka cosankhika ca Ambuye. (Luka 4:18-19)

za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Machitidwe 10:38)

Ma vesi awa apereka mndandanda wa zolinga za kudzodzedwa ndi cholinga chokagwira ntchito.

Kudzodza kumapangitsa:

- Kulalikira Uthenga Wabwino.
- Kutumikira ena.
- Kuchiritsa amene asweka mtima.
- Kuchiritsa amene akudwala kuthupi. (Onaniso Yakobo 5:14-15 ndi Marko 6:13)
- Kulalikira kumasulidwa kwa onse amene amangidwa mu uzimu.
- Kutsekula maso a onse amene ali akhungu mu uzimu.
- Kuwamasula onse amene atunduzidwa, kuvulazidwa ndi mdani.
- Kulalirika chaka chovomerezeka ndi Ambuye. (Onaniso 2 Akorinto 6:2)
- Kupita ndikukachita zabwino.
- Kuchilitsa onse amene akuzuzidwa ndi ziwanda.

UDINDO:

Mulungu amadzodza okhulupirira ndi udindo wauzimu. China chirichonse chimene wakudalirani nacho, kaya mchachikulu kapena chaching'ono, sichinabwere chifukwa chakuthekera kwanu.

Sichifukwa chamaphunziro anu, umunthu wanu kapena udindo. Mumalandira udindo wa uzimu chifukwa chakudzodza:

Ndipo Yehova ananena ndi Aroni, Ndipo taona, Ine ndakupatsa udikiro wa nsembe zanga zokweza, ndizo zopatulika zonse za ana a Israyeli; cifukwa ca kudzozedwaku ndazipereka kwa iwe, ndi kwa ana ako amuna, likhale lemba losatha. (Numeri 18:8)

MALANGIZO:

Kudzodza kumakuphunzitsani kuti:

Ndipo inu, kudzoza kumene munalandira kucokera kwa iye, kukhala mwa inu, ndipo simusowa kuti wina akuphunzitseni; koma 9 monga kudzoza kwace kukuphunzitsani za zinthu zonse, ndipo kuli koono, sikuli bodza ai, ndipo monga kudaphunzitsa inu, mukhale mwa iye. (1 Yohane 2:27)

Izi sizikutanthauza kuti simukuyenera kulandira chiphunzitso cha mmalemba kuchokera kwa ena. Mulungu anapatula ena mumpingo kuti akhale aphunzitsi pa cholinga chimenechi (Aefeso 4:11). Mzimu Woyera anawadzodza iwo kuti akaphunzitse Mau a Mulungu. Koma ngati mulibe mwayi oti mkulandirako utumiki wa anthu oterewa amene asakhidwa ndi Mulungu, ndekuti kudzoza kwa Mulungu kupitiriza kukuphunzitsanibe.

Kudzodza kumakuthandizani inu kuti mukasathule choonadi chachiphunzitso chomwe mukuva kuchokera kwa ena. Kumawonetseraso choonadi chimene inu simukuchivetsetsa ndipo kumatsekulaso mabvumbulutso a Mulungu olembedwa mau kwa inu. Zindikirani kuti kudzoza kumatiphunzitsa ife “zinthu zonse.” Muli mphamvu mukudzodza imene imakutsogolerani inu mbali iriyonse ya moyo wanu ndi utumiki.

KUKHALABE:

Kudzodza kwa Mulungu kumakupangitsani inu kuti mukhalebe mwa Yesu. Dziwani kuti gawo la vesi iyi yomwe mwangophunzira:

Ndipo inu, kudzoza kumene munalandira kucokera kwa iye, kukhala mwa inu, ndipo simusowa kuti wina akuphunzitseni; koma monga kudzoza kwace kukuphunzitsani za zinthu zonse, ndipo kuli koono, sikuli bodza ai, ndipo monga kudaphunzitsa inu, mukhale mwa iye. (1 Yohane 2:27)

Ndi chinthu chimodzi kulandira Yesu ngati mpulumutsi. Ndi chinaso kuphunzira kukhalabe mwa Iye ndikuyenda mkumvera Mau Ake ndi chifuniro Chake. Kudzoza kumakuphunzitsani kuti muzichita zimenezi.

UFULU:

Goli la ukapolo limawonegwedwa ndi kudzoza. Magoli amkagwiritsidwa ntchito kale kale pomangirira nyama pamodzi kuti zigwire ntchito mminda. Maiko ena akugwiritsidwabe ntchito pazifukwa zomwezo lero. Yesu anayakhulapo zagoli pamene anati:

Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu. Senzani gori langa, ndipo phunzirani kwa Ine; cifukwa ndiri wofatsa ndi wodzicepetsa mtima: ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu. Pakuti 1 gori langa liri lofewa, ndi katundu wanga ali wo pepuka. (Mateyu 11:28-30)

Tonsefe tiri pansu pagoli la mtundu womwewu. Kodi Muli pansu pa goli la satana kapena la Mulungu. Goli la ukapolo la satana lili ndi magawo atatu:

1. Goli la tchimo:

Ine ndine Yehova Mulungu wanu, amene ndinakuturutsani m'dziko la Aigupto, kuti musakhale akapolo ao; ndipo ndinatyola mitengo ya magoli anu, ndi kukuyendetsani coweramuka. (Levitiko 26:13)

“Goli la ku Igupto” likuthanthauza kuti goli la uchimo. Goli iri likuyenera kuphwanyidwa ngati mwabwera pansu pa goli la Yesu.

2. Goli la nokha:

Paulo amkalimbana ndi goli la yekha:

Pakuti cimene ndicita sindicidziwa; pakuti sindicita cimene ndifuna, koma cimene ndidana naco, ndicita ici. (Aroma 7:15)

3. Goli la munthu:

Goli la munthu ndi ukapolo omwe umaikidwa pa inu ndi anthu ena.

Inde, amanga akatundu olemera ndi osautsa ponyamula, nawasenza pa mapewa a anthu; koma iwo eni okha safuna kuwasuntha amenewo ndi cala cao. (Mateyu 23:4)

Goli la munthu ndikuphatikizapo ukapolo wopalamula, chikhalidwe, chipembedzo, kapena kumakhala chikhalidwew chosatheka choikidwa ndi ena. Kodi maukulu amenewa angaphwasulidwe bwanji mmoyo wanu ndi mmiyoyo ya onse amene ali mu utumiki? Amaphwasulidwa ndi kudzodza.

Ndipo padzakhala tsiku lomwelo, kuti katundu wace adzacoka pa phewa lako, ndi gori lace pakhosi pako; ndipo gori lidzathedwa cifukwa ca kudzoza mafuta. (Yesaya 10:27)

Simungaphwasule goli la satana podalira mphamvu zanu. Simungapange izi podalira mau anu anzeru. Goli lililonse limaphwasulidwa ndi kudzodza.

CHIMWEMWE:

Yesu anadzodzedwa ndi mafuta achimwemwe:

Koma ponena za Mwana, ati, Mpando wacifumu wanu, Mulungu, ufikira nthawi za nthawi; Ndipo ndodo yacifumu yoongoka ndiyo ndodo ya ufumu wanu. Mwakonda cilungamo, ndi kudana naco coipa; Mwa ici Mulungu, ndiye Mulungu wanu, wakudzozeni Ndi mafuta a cikondwerero ceni ceni koposa anzanu. (Ahebri 1:8-9)

Onse amene amakonda chiyero ndipo amadana ndi zoipa azadzodzedwa ndi chimwemwe chomwecho. Kudzodza kwa Mulungu kumabweretsa chimwemwe choposa m'moyo mwanu. Chimwemwe cha Mulungu ndi mphamvu imene imalimbikitsa ntchito yanu imene mumanchitira Mulungu.

KUDZODZA KWA PADERADERA

Zolinga za kudzodza uku mwangophunziraku ndi kwa okhulupirira onse. Koma Mulungu amadzodzaso anthu mwapaderadera chifukwa cha utumiki ndi ntchito yapaderadera imene apatsidwa. Ena amadzodzedwa ngati atumwi, ena ngati aphunzitsi. Ena ndi abusa pamene ena ndi aneneri. Pali kudzodza kosiyanasiyana kwa Mulungu kumene amapereka kwa okhulupirira.

Yesu anali ndi kudzodza kwapaderadera kuti azafere machimo a anthu. Dzina loti “Kristu” limatanthauza kuti “odzodzedwa.” Dzina la Yesu limatanthauza “Mpulumutsi.” Pamene dzina loti “Yesu Kristu” lagwiritsidwa ntchito, limatanthauza kuti ndi odzodzedwa wa Mulungu kuti akhale Mpulumutsi wa dziko. Isanafike imfa Yake, mkazi wina anamudzodza Yesu ndi mafuta amtengo wapatali kwambiri. Yesu anati:

Pakuti mkaziyo, m'mene anathira mafuta awa pathupi panga, wandicitiratu ici pa kuikidwa kwanga. (Mateyu 26:12)

Yesu amkadziwa kuti wadzodzedwa ndi Mulungu kuti akafe chifukwa cha machimo a anthu. Palibe munthu wina aliyense anakhalapo ndi kudzodza kwa mtundu umenewu.

Kupyolera mu zolembedwa m'Baibulo, Mulungu anadzodza anthu chifukwa cha utumiki wapaderadera (Onani 2 Mbiri 22:7). Pamena anthu amkayesera kutenga utumiki wapaderadera

popanda kudzodza kwa Mulungu, akangochita choncho mabvuto amkayambiranso. Werengani nkhani ya Miriam ndi Aroni mu Numeri 12 monga chitsanzo chachimenechi. Miriam ndi Aroni ngakhale anali ndikudzodza kofanana ndi kwa Mose ndipo amkatha kutsogolera Israeli moyenera . Koma panali kusiyanabe. Chitsanzo china chikupezeka pa Numeri 16 mu nkhani ya Kora amene anayesera kutenga kudzodza kofanana ndi kwa Mose.

Kugawanikana komwe kulipo mu nthupi la Kristu kukubwera kuchokera kwa anthu amene amayesera kupita mu utumiki umene sanalandirire kudzodza kwake. Koma otsanzirawa sakhala ndizotsatira za mphamvu. Amadabwa kuti vuto ndi chani. Amachita zinthu chimodzimodzi ngati wina wake koma zotsatira zake zimakhala zosiyana. Yankho lake limapezeka mu mphamvu yakudzodza. Kudzodza kwa Mulungu kumakhala pa munthu chifukwa cha ntchito yapaderadera imene wapatsidwa, osati pa wina aliyense. Chifukwa cha ichi, wina amapambana pamene wina amalephera.

Mwa tchimo limodzi lathupi lomwe analembedwa pa Agalatiya 5:20 ndilotchedwa kuti “kutengera.” Kutengera ndi nchitidwe wakaduka omwe umawonetseredwa pokopera ena. Mulungu sangadalitse okopera. Mulungu akufuna onse amene angatuluke mutchimo lokopera kulowa mu bvumbulutso kupyolera mu mpamvu yodzodza.

KODI MUNGALANDIRE BWANJI KUDZODZA?

Kodi mungalandire bwanji mphamvu yakudzodzayi?

KUZINDIKIRA KOMWE IKUCHOKERA:

Monga momwe mwaphuzira mu phunziro lino, kochokera kudzodza kwa mphamvu za uzimu ndi kwa Mulungu. Simungakhulupirire maphunziro anu, umunthu, kapena kudziwika kwana.

Simungalandire kudzodza kwana kuchokera kwa wina aliyense.

Palibe chomwe mungachite kuti mulandire kudzodza kumeneku. Simungalandire chifukwa cha maimvaimva. Mulungu nde chiyambi cha kudzodza kwa uzimu. Kuti mulandire kudzodza kumeneku, choyamba mukuyenera kuzindikira kaye komwe imachokera.

KUBADWANSO MWATSOPANO:

Chifukwa chakuti iyi ndi mphamvu ya uzimu imene imayenda kuchokera kuchiyambi kwa Mulungu, mukuyenera kukhala obadwanso mwatsopano mu uzimu kuti mulandire kudzodzaku. Chifukwa chake ndi ichi:

**Koma munthu wa cibadwidwe ca umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu:
pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira, cifukwa ziyesedwa mwauzimu.
(1 Akorinto 2:14)**

Kudzodza kwa mphamuku kumayenda kuchokera kwa Mzimu wa Mulungu. Nde munthu wochimwa sangalandire. Simungalandire pokhapokha ngati ndinu munthu wauzimu.

KUMAWERENGA MAU A MULUNGU NDI KUPEPHERA:

Chifukwa chakuti Mulungu nde kochokera kwakudzodza, mukuyenera kukhalabe mkulumikizana ndi Iye kupyolera mupephero (mmene mumayakhula Naye) ndi Mau a Mulungu (kupyolera mmene Iye amayakhula kwa inu). Mmomwe inu mukukhalira mau Ake, ndi meneso iwo akukhalira mwa inu, mmenemoso kud zodza kochulukira kuzayenda mmoyo mwanu.

KUPHWASULA GOLI:

Mwaphunzira mu chaputala chino kuti cholinga chimodzi cha kud zodza ndi kuphwanya magoli a ukapolo. Mupempheni Mulungu kuti apwanye goli lililonse la uchimo, lanokha, kapena limene laikidwa ndi anthu ena. Mukuyenera kukumana ndi kud zodza kumene kumapwanyanya goli mu mmoyo mwanu lisanafalikire kwa ena kudutsira mwa inu.

KULANDIRA MZIMU WOYERA:

**za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi
mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi
ndierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Machitidwe 10:38)**

Vesi imeneyi ikuwonetsera mmene kud zodza kwa Mulungu kumagwirizanirana ndi kugwira ntchito kwa mphamvu ya Mzimu Woyera mmoyo mwanu. Kuti mukumane ndi mphamvu yakudzodza, mukuyenera kulandira Mzimu Woyera. Mwaphunzira kale pa zazimenezi mu chapulatala 8 pa mutu wa “Mphamvu ya Mzimu Woyera.”

MUSAMAYIKE CHIDWI PAZOFOOKA ZANU:

Anthu ambiri amaika chidwi chawo pazofooka zawo osati pa zakuthekera komwe kuli mwa iwo kupyolera mu kud zodza kwa mphamvu. Mfumu Davide nthawi ina anati:

**Mulungu alange Abineri, naonjezepo, ndikapanda kumcitira Davide monga Yehova
anamlumbirira; (2 Samueli 3:39)**

Davide anazindikira kuti payekha ndi ofooka, ngakhaletu kuti anali mfumu. Mphamvu imene anakumana nayo inabwera kudzera mukudzodza. Inasitha kufooka kwake kukhala mphamvu. Sanaike chidwi pa zofoka zake, koma pakuthekera kwake kupyolera mu mphamvu ya kudzodza. Ichi nchifukwa chake anakwanitsa kunena kuti:

Pakuti mwa Inu ndipyola khamu la anthu; Ndipo mwa Mulungu wanga ndilumphira linga. (Salimo 18:29)

Ophunzira a Yesu anali anthu poyamba amantha komaso osakhulupirira. Onse anamuthawa Yesu munthawi yake yovutika. wina anachita kumukana kuti samamudziwa. Nde ndigulu lomweri limene Yesu analipatsa ntchito yokafikira dziko lonse ndi Uthenga Wabwino. Yesu sanaike chidwi chake pa zifooko zawo. Sanayang'ane kusaphunzira kwao, kapena kusatchuka kwao. Sanayang'ane mbiri yawo mmene anakhalira akulepherera mbuyomu. Anawona chomwe angakhale pamena angalole kuti mphamvu yakudzodza kuti isithe miyoyo yawo. Anawona mmene atakhalire akalandira Mzimu Woyera.

Lekani kuika chidwi pa inu eni. Zindikirani kuti Mzimu wa Mulungu uli mwa inu. Ndi ntchito Yake, utumiki Wake, zozizwa Zake, Kudzodza Kwake. Mupepheni kuti kudzodza kuyende mwa inu. Yambani kufikira ena mu utumiki, ndipo muzayamba kumva kuyenda kwa mphamvu mwa inu.

Mulungu sangangokudzodzani kuti mungokhala chabe mumipando ya mkachisi. Kudzodza kwa mphamvu kumaperekedwa ndi zolinga chapaderadera zomwe mwaphunzira mu chaputala 6. Pamena mukuika mphamvu zanu pa zolingazi, ndi pameneso kudzodza kwa mphamvu kuzayende mwainu mocholuka.

KUZINDIKIRA KUDZODZA KWANU KWAPADERADERA:

Kuti muike chidwi chanu pa kudzodza kwa paderadera mu utumiki, mukuyenera kuzindikira mphatso ya Uzimu imene Mulungu wakupatsani. Onani pa zimenezi mu bulu la sukulu ya Harvestite Institute lotchedwa “*Utumiki wa Mzimu Woyera*,” kuti mupeze chitsogozo pa nkhani imeneyi.

MALO OMWE ODZODZEDWA AMAKHALAPO

Kukhala odzodedwa ndi Mulungu kumakuikani inu patsogolo peni peni pa nkondo ya uzimu. Baibulu laulula kuti onse amene adzodzedwa ndi mphamvu ya Mulungu azakumana ndichitsutso

Masalmo 2:3 Tidule zomangira zao, Titaye nsinga zao. (Salimo 2:2-3)

Davide anati:

Cimene adani anu, Yehova, atonza naco; Cimene atonzera naco mayendedwe a wodzozedwa wanu. (Salimo 89:51)

Koma Mulungu anayakhulapo za onse amene amalimbana ndi odzozedwa Ake:

Wokhala m'mwambayo adzaseka; Ambuye adzawanyoza. Pomwepo adzalankhula nao mu mkwiyo wace, Nadzawaopsa m'ukali wace: (Salimo 2:4-5)

Mulungu ndi mphamvu yanu pamene mwakumana ndi chitsutso chimenecho:

Yehova ndiye mphamvu yao, Inde mphamvu ya cipulumutso ca wodzozedwa wace. (Salimo 28:8)

Tsopano ndidziwa kuti Yehova apulumutsa wodzozedwa wace; Adzambvomereza m'Mwamba mwace moyera Ndi mphamvu ya cipulumutso ca dzanja lace lamanja. (Salimo 20:6)

Muzikhala osamalitsa pazimene mukunena zokhudzana ndi okhulupirira odzozedwa.

Muziwapatsa ulemu odzozedwa onse amene ali pamwamba panu. Mulungu amaitenga mphamvu yakudzozedwa mwachidwi.

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Kodi cholinga cha kudzodza koyera mu Chipangano Chakale ndi chiani?

3. Palekani zitsanzo zamomwe kudzodza koyera kumkagwiritsidwira ntchito mu Chipangano Chakale.

4. Kodi dzina loti “Kristu” limatanthauza chani”?

5. Lembani mwachidule zimene mwaphunzira zokhuzana ndi zolinga za mphamvu ya kudzodza.

6. Kodi mkofunika bwanji kuti muzindikire kudzodza kwanu kwapaderadera mu utumiki?

7. Kodi mungalandire bwanji kudzodza kwa mphamvu?

8. Kodi chiyambi cha kudzodza kwa Uzimu ndi ndani?

(Mayankho amayesowa aperekedwa Kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Phunzirani kwambiri zokhudzana ndi zolinga za kudzodza kwa Uzimu mu Chipangano Chakale.
 - Kudzodzedwa kwa amseme: Levitiko 8:12,30; Eksodo 28:41; 29:7; 30:30
 - Kudzodzedwa kwa Kachisi ndi zonse zokhalamo: Eksodo 20:22-29; 40:9-11
 - Kudzodzedwa kwa mafumu. Pali zolembedwa zambiri pa za izi. Mwachitsanzo onani 1 Samueli 19:16; 20:1; 16:1, 12, 13; 2 Samueli 2:7; 1 Mafumu 1:33-34
2. Satana nthawi ina yake anadzodzedwapo ndi Mulungu. Werengani zokhuzana izi pa Ezekeli 28:14
3. Chifukwa chakuti ndinu odzodzedwa wa Mulungu sizikutanthuza kuti ndinu opatulika kuchilango cha tchimo. Onani Salimo 89:38
4. Mulungu amayang'ana khope za onse odzodzedwa Ake ndipo amasamala za iwo (Masalimo 89:9). Amawonetsera chifundo kwa iwo (Masalimo 18:50)
5. Mfumu Davide anamvetsetsa kufunika kosachitira choipa odzodzedwa ake a Mulungu. Onani 1 Samueli 24 ndi 26 ndi 2 Samueli 1:16,21
6. Chaputala ichi chapereka mndandanda wa zolinga za kudzodza monga kuti kumaperekera mphamvu kwa okhulupirira chifukwa cha utumiki. Sathulani utumiki wanu molingano ndi zolinga zimenezi. Ndi zingati zimene ziri mu utumiki wanu?
 - Kulalikira Uthenga Wabwino.
 - Kutumikira osauka.
 - Kuchiritsa odwala kunthupi.
 - Kuchiritsa onse osweka mitima.
 - Kulalikira kumasukidwa kwa onse amene amangidwa ndi magoli auzimu.
 - Kutsekula maso kwa onse amene ali akhungu mu uzimu.

- Kumasula onse amena atunduzidwa, avulazidwa ndi mdani.
- Kulakira chaka chomvomerezeka cha Ambuye
(Onani 2 Akorinto 6:2. Izi zimanthauza unthenga wachipulutso)
- Kupita ndikukachita zabwino.
- Kuchiritsa onse amene akuponderezedwa ndi ziwanda.

CHAPUTALA 11

NDONDOMEKO YA MPHAMVU 5:

MPHAMVU, CHIKHULUPIRIRO, NDI NTCHITO

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

Kulemba vesi yotsogolera osawonera.

- Kupereka tanthauza la chikhulupiro.
- Kuloza milingo ya chikhulupiro.
- Kupereka mitundu yachikhulupiro.
- Kufotokoza mmene chikhulupiro chingakulire.
- Kulemba mwachidule ngwirizano pakati pa mphamvu, chikhulupiro ndi ntchito.

VESI YOTSOGOLERA:

Ndipo Stefano, wodzala ndi chisomo ndi mphamvu anachita zozizwa ndi zizindikilo zazikulu mwa anthu. (Machitidwe 6:8)

MAU OYAMBA

Mu Mateyu 17, ophunzira anayesera kutulutsa chiwanda mwa mwana, koma analephera.

Pamene anamubweretsa kwa Yesu, Iye anakwanitsa kumuchiritsa mwanayo.

Ophunzira anamufunsa Yesu, “Nchifukwa chani sitinakwanitse kutulutsa chiwandacho?” Yesu anayakha...

pakuti anawaphunzitsa monga mwini mphamvu, wosanga alembiao. (Mateyu 17:29)

Pazomwe zinachitikazi Yesu anagawana nao ndondomeko yofunika ya mphamvu ya Uzimu.

Mphamvu ikuyenera kugwira ntchito muchikhulupiro kuti ikathe kugwira ntchito ya Mulungu.

Chikhulupiro mwa munthu ndi kumvomera kwa mphamvu ya Mulungu:

Ndipo Yesu ananena naye, Ngati mukhoza! Zinthu zonse zitheka ndi iye wakukhulupirira. (Marko 9:23)

Chaputala ichi chikukamba za ngwirizano wapakati pa mphamvu, chikhulupiriro ndi ntchito.

TANTHAUZO

Chikhulupiriro chimatanthauza kukhulupirira ndi kukhala ndi chitsimikizo pa chinthu china chake. Kukhulupirira kumatanthauza kuti kutsimikizika mtima. Mau oti “chikhulupiriro, kukhulupirira, ndi kutsimikizika mtima” zonsezi zimatanthauza chinthu chimodzi Mmalemba.

Baibulo limachifotokoza chikhulupiro ngati:

Koma cikhulupiriro ndico cikhazikitso ca zinthu zoyembekezeka, ciyesero ca zinthu zosapenyeka. (Ahebri 11:1)

Chikhulupiriro chimaperaka chitsimikizo kuti zinthu zolonjezedwa za mtsogolo ndi zoonza ndikutiso zinthu zosaoneka ziri zenizeni.

Chikhulupiriro sichimodzimodzi ngati “maganizo opambanira zinthu” amene amaphunzitsidwa ndi zipembedzo zina. “Maganizo pa zinthu” amaphunzitsa kuti munthu apambane mavuto onse mu dziko lenileni (Dziko la zinthu) pogwiritsa ntchito maganizo. Chiphunzitsa ichi chimakhazikika pa munthu. Chimaika chidwi pa munthu mwini osati pa Mulungu. Ganizo limeneri silimakhazikika pa Mulungu, koma pa munthu. Chikhulupiriro sichinthu chimene munthu angapange pakudzera mukuyesetsa kwa maganizo ake.

Chikhulupiriro chimene Baibulo limanena sichikhulupiriro cholengedwa chimene chimakhulupirira zinthu zolengedwa za kudziko lapansi chomwe umaphunzira pokumana ndi zinthu zowoneka. Mwachitsanzo, chikhulupiriro chakuti mpando omwe mwakhalawo ukuthandizirani kuti musagwe.

MITUNDU YACHIKHULUPIRIRO IMENE ILI M’BAIBULO

Pali mitundu yosiyanasiyana imene imakambidwa mmalemba:

CHIKHULUPIRIRO CHOPULUMUTSA:

Popeza tsono tayesedwa olungama ndi cikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Kristu; (Aroma 5:1)

Chikhulupiriro chopulumutsa chimakhudzana ndi kulapa kweni kweni kwa tchimo. Mukuyenera kumva, kukhulupirira, ndiponso panokha kulandira Uthenga Wabwino. Chikhulupiriro chopulumutsa chimafuna kuti munthu avomereze Mulungu.

Chikhulupiriro ndi mphatso yochokera kwa Mulungu imene imapangitsa kuti anthu apulumuke.

Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu; (Aefeso 2:8)

Simungapululumuke popanda chikhulupiriro:

Amene akhulupirira nabatizidwa, adzapulumutsidwa; koma amene sakhulupirira adzalangidwa. (Marko 16:16)

koma wopanda cikhulupiriro sikutheka kumkondweretsa; pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti alipo, ndi kuti ali wobwezera mphotho iwo akumfuna iye. (Ahebri 11:6)

CHIKHULUPIRIRO CHOYERETSA:

Ndinapacikidwa ndi Kristu; koma ndiri ndi mayo; wosatinso ine ai, koma Kristu ali ndi moyo mwa ine; koma moyo umene ndiri nao: tsopano m'thupi, ndiri nao m'cikhulupiriro ca Mwana wa Mulungu, amene anandikonda, nadzipereka yekha cifukwa ca ine. (Agalatiya 2:20)

Chikhulupiriro choyeretsa chimakuyenerezani inu kuti mukhale moyo woyera mutalandira Yesu monga mpulutsi. Mukuyenera kukumana ndi chikhulupiriro chopulumutsa ndi cholinga choti mulandire chikhulupiriro choyeretsa.

CHIKHULUPIRIRO CHOTETEZA:

Chikhulupiriro ndi chida chozitetzera kumdani wanu wa uzimu, satana.

koposa zonse mutadzitengeranso cikopa ca cikhulupiriro, cimene mudzakhoza kuzima naco mibvi yonse yoyaka moto ya woipayo. (Aefeso 6:16)

Satana azalimbana ndi chikhulupiriro chanu potumiza mivi yosakhulupirira mmaganizo mwanu. Chikhulupiriro mwa Mulungu chimapereka chitetezo cha uzimu ku ziwembu ngati izi.

MPHATSO YA CHIKHULUPIRIRO:

Pali mphatso ya uzimu ya chikhulupiriro yoperekedwa ndi Mzimu Woyera:

Pakuti kwa mmodzi kwapatsidwa mwa Mzimu mau a nzeru; koma kwa mnzace mau a cidziwitso, monga mwa Mzimu yemweyo: kwa wina cikhulupiriro, mwa

Mzimu yemweyo; ndi kwa wina mphatso za maciritso, mwa Mzimu mmodziyo; (1 Akorinto 12:8-9)

Munthu wokhala ndi mphatso yachikhulupiriro ya uzimu amakhala ndikuthekera kwapadera kokhulupirira Mulungu. Amadziwa kuti Mulungu achita zosatheka. Amagwiritsa ntchito chikhulupiriro chimenechi ngakhale ena omuzungulira asakukhulupirira.

CHIPATSO CHA CHIKHULUPIRO:

Chikhulupiriro sichinthu choti mungachikhazikitse mwanokha. Ndi chipatso cha uzimu choikidwa mmoyo mwanu ndi Mzimu Woyera.

Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, icikhulupiriro, (Agalatiya 5:22)

Chikhulupiriro monga chipatso chachikhalidwe ndi malingaliro achikhulupiriro amene tiri nawo pa Mulungu

MLINGO WA CHIKHULUPIRO

Baibulo limaonetsa kuti pali kusiyana kwa mlingo wachikhulupiriro. Yesu anayakhulapo za anthu amene samagwiritsa ntchito chikhulupiriro chawo kuti ndi anthu opanda chikhulupiriro (Mateyu 17:17). Iye anayakhulapo pa za omwe ali ndichikhulupiriro chochepa (Mateyu 6:30; 8:26; 14:31; Luka 12:28) koma za omwe ali ndi chikhulupiriro chachikulu (Mateyu 8:10; 15:28; Luka 7:9)

Baibulo limaphunzitsa kuti munthu aliyense ali ndi mlingo wake wachikhulupiriro omwe waperekedwa kwa iye ngati mphatso kuchokera kwa Mulungu:

Pakuti ndi cisomo capatsidwa kwa ine, ndiuza munthu ali yense wa inu, kuti asadziyese koposa kumene ayenera kudziyesa; koma aganize modziletsa yekha, monga, Mulungu anagawira kwa munthu ali yense muyeso wa cikhulupiriro, (Aroma 12:3)

CHIKHULUPIRO CHINGAKULE BWANJI?

Baibulo limatiuza mmene chikhulupiriro chingakulire:

Comweco cikhulupiriro cidza ndi mbiri, ndi mbiri idza mwa mau a Kristu. (Aroma 10:17)

Chikhulupiriro chanu chimakula pakumva Mau a Mulungu. Chikhulupiriro chopulumutsa chimabwera pakumva Mau a Mulungu. Koyambirira mukuyenera kumva mau a Mulungu kuti mukathe kulapa tchimo ndi kulandira Yesu monga Mpulumutsi. Simungakumane ndi mphamvu ya uzimu pokhapokha mutakuman kaye ndi chikhulupiriro chopolumutsa.

Mukapulumsidwa, chiphunzitso ndi kulalikidwa kwa Baibulo kumakulitsa chikhulupiriro chanu. Kuchuluka kwakumva mau a Mulungu kumagwirizana ndi kuchulukaso kwa chikhulupiriro chanu mmene chikulire. Chikhulupiriro chimenechi chimapitiriza kukupangani inu kuti mufanane ndi Yesu.

Kuyeretsedwa ndikukhala moyo wachiyero. Mukuyenera kukhala nchiyero kuti mukumane ndi mphamvu ya uzimu. Kupitirira kukhalabe muuchimowadala kumatchinga kuyenda kwa mphamvu ya Mulungu mmoyo wanu.

Pamene chikhulupiriro chikukula kwambiri, kuzakhala kosavuta kwa inu kukhala moyo wachiyero ndi kuziteteza ku chiwembu cha mdani waku uzimu. Akhristu opanda mphamvu amakhala ogonjetsedwa kale.

chikhulupiriro chepa chimakhala cha mphamvu kwambiri:

Ndipo Iye ananena kwa iwo, Cifukwa cikhulupiriro canu ncacing'ono: pakuti indetu ndinena kwa inu, Mukakhala naco cikhulupiriro monga kambeu kampiru, mudzati ndi phiri ili, Senderapo umuke kuja; ndipo lidzasendera; ndipo palibe kanthu kadzakulakani kosacitika. [(Mateyu 17:20)

CHIKHULUPIRIRO, NTCHITO, NDI MPHAMVU

Ndikosavuta kuwona mmene chikhulupiriro chimakhudzira kayendedwe ka mphamvu ya Mulungu mmoyo mwanu. Kopanda chikhulupiriro, muli pangozi yongomvera mau wamba opanda mphamvu ili yonse.

Pakuti kwa ifenso walalikidwa Uthenga Wabwino, monganso kwa iwo; koma iwowa sanapindula nao mau omvekawo, popeza sanasanganizika ndi cikhulupiriro mwa iwo amene adawamva. (Ahebri 4:2)

Koma paliso kugwirizana kwakukulu pakati pa chikhulupiriro, ntchito ndi mphamvu. Kuti mukumane ndi mphamvu, mukuyenera kukhala ndi chikhulupiriro. Kuti muwonetsere mphamvu mukuyenera kukhala ndi chikhulupiriro. Pakuti chikhulupiriro ndi mphamvu kuti zikhale zaphindu pakufalitsa Uthenga Wabwino, zikuyenera kuwonetseredwa ndi ntchito. yakobo abalemba:

Cipindulocace nciani, abale anga, munthu akanena, Ndiri naco cikhulupiriro, koma alibe nchito? Kodi cikhulupiriroco cikhoza kumpulumutsa? Momwemonso cikhulupiriro, cikapanda kukhala nazo nchito, cikhala cakufa m'kati mwacemo. Koma wina akati, Iwe uli naco cikhulupiriro, ndipo ine ndiri nazo nchito; undionetse ine cikhulupiriro cako copanda nchito zako, ndipo ine ndidzakuonetsa iweikhulupiriro canga coturuka m'nchito zanga. Pakuti monga thupi lopanda mzimu liri lakufa, koteronso cikhulupiriro copanda nchito ciri cakufa. (Yakobo 2:14, 17-18, 26)

Chikhulupiriro ndi ntchito ndi zongwirizana moyandikana monga mzimu ndi nthupi:

Sitifano anali wodzala ndi chikhulupiriro ndi mphamvu zomwe zinampangitsa iye kuchita ntchito zazikulu.

Ndipo Stefano, wodzala ndi cisomo ndi mphamvu, anacita zozizwa ndi zizindikilo zazikuru mwa anthu. (Machitidwe 6:8)

Kukatero tikupemphereraninso nthawi zonse, kuti Mulungu wathu akakuyeseni inu oyenera kuitanidwa kwanu, nakakwaniritse comkomera conse, ndi nchito ya cikhulupiriro mumphamvu; Ntchito zachikhulupiriro zimachitika ndi mphamvu: (2 Atesalonika 1:11)

Mulungu amafuna kuchita ntchito ya chikhulupiriro ndi mphamvu kupyolera mwa inu. Pamene mukugwiritsa ntchito chikhulupiriro, chimalumikizana ndi mphamvu ya Mulungu ndi ntchito zanu. “Zinthu zonse ndi zotheka,” Yesu anati, “kwa iye amene akhulupirira!”

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Perekani tanthauzo lachikhulupiriro lochokera m'Baibulo.

3. Lozani milingo ya chikhulupiriro imene Yesu anayakhula.

4. Lembani mitundu yachikhulupiriro imene takambirana mu phunzirori.

5. Kodi chikhulupiriro chingakule bwanji?

6. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira mu chaputala chino zokhuzana gwirizano wapakati pa mphamvu, chikhulupiriro ndi ntchito.

(Mayankho amayesowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Pitirizani kuphunzirabe zokhudzana chikhulupiriro powerenga Ahebri 11 chomwe chimatchulidwa kuti “Chaputala chachikhulupiriro” cha Baibulo. Lembani wachidule zomwe mwaphunzira zokhudzana mphamvu ya chikhulupiriro kuchokera ku zitsanzo zimenezi:

2. Chitsanzo chimodzi chachikulu chachikulupiriro chomwe chiri mu Baibulo ndi Abrahamu.

- Abrahamu analungamitsidwa ndi chifukwa chachikhulupiriro: Yakobo 2:23
- Chikhulupiriro chake chinampatsa chitsimikizo cha malonjezano a Mulungu: Aroma 4:18-21
- Mulungu anapeza mtima wa Abrahamu okhulupirika: Nehemiya 9:8
- Okhulupirira amene anatsata chitsanzo chake ndi anthuso achikhulupiriro: Aroma 4:11-12

Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira zokhudzana ndi Abrahamu muma vesi awa:

CHAPUTALA 12
NDONDOMEKO YA MPHAMVU 6:
MPHAMVU MUDZINA LA YESU

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osawonera.
- Kufotokoza kufunika kwa maina munthawi ya Baibulo.
- Kuloza dzina lalikulu lomwe liri pamwamba pa maina onse.
- Kupereka tanthauzo la dzina la “Yesu.”
- Kufotokoza momwe Yesu analandirira dzina Lke.
- Kufotokoza chotsogozo cha Baibulo momwe tingawiritsire ntchito dzina la Yesu.

VESI YOTSOGOLERA:

Mwa ichinso Mulungu anamkwezetsa Iye, nampatsa dzina limene liposa maina, kuti m'dzina la Yesu bondo liri lonse lipinde, la za m'mwamba ndi zapadziko, ndi za pansu pa dziko, ndi malilime onse abvomereze kuti Yesu ndi Ambuye, kuchitira ulemu Mulungu Atate. (Afilipi 2:9-11).

MAU OYAMBA

Mwaphunzira za mphamvu ndi ulamuliro operekedwa ndi Mulungu kwa Yesu Kristu ndi momwe Yesu anaperekera mphamvu yomweyi ndi udindo omwewu kwa okhulupirira. Imodzi mwandondomeko za mphamvu ya uzimu ndi kugwiritsa ntchito dzina lake lomwe. Chaputala ichi chikhazikika pa mphamvu imene ili mu dzina la Yesu.

KUFUNIKA KWA MAINA

Munthawi ya Baibulo maina anali ofunika kusiyana ndi lero. Muchikhalidwe chamakono ano dzina limangogwiritsidwa ntchito ngati loitanira munthu chabe. Munthawi ya Baibulo, kufunika kwakukulu kumkaphatikizidwa ku dzina . Dzina loperekedwa kwa munthu kawirikawiri

limawonetsera zimene zinali pa nthawi imene amkabadwa (Genesis 19:22). Nthawi zina dzina limapereka chiyembekezo kapena uneneri (Yesaya 8:1-4; Hoseya 1:4)

Chifukwa chakufunika kwa maina munthawi ya Baibulo, Mulungu anasitha maina a anthu ambiri. Anasitha dzina la Abramukukhala Abrahamu chifukwa chatsogolo lake.

Sudzachedwanso dzina lako Abramukukhala Abrahamu; cifukwa kuti ndakuyesa iwe atate wakhamu lamitundu. (Genesis 17:5)

Dzina loti Abrahamu limatanthuza kuti “Tate wamafuko opambana.” Mulungu anasithaso dzina la Sarai kukhala Sara ndi Yakobokukhala Israeli pachifukwa chofanana. Mu Chipingano Chatsopano nchitidwewu unapatiriraso. Simoni anatchulidwa “Petro” ndi Saulo anakhala “Paul.” Maina awo amkawonetsera tsogolo lao mudongosolo la Mulungu.

Chifukwa cha kufunika kwa tanthauzo lamaina, Mulungu anasakha dzina lapaderadera la Mwana Wake.

DZINA LA YESU

Dzina la Yesu linaperekedwa kwa Mwana wa Mulungu mmene anabwera kudziko lapansi mu umunthu. Linaperekedwa pakumvera lamulo lamngelo kwa Yosefe, mamuna wa Mariya, amake a Yesu:

Ndipo adzabala mwana wamwamuna, ndipo udzamucha dzina lace Yesu; pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ace kumacimo ao. (Mateyu 1:21)

Dzina loti “Yesu” liamatanthauza kuti “Mpulumutsi.” Yesu analinso ndi maina ena. Nthawi zambiri amangotchulidwa kuti Yesu Kristu, Ambuye Yesu, ndi Ambuye. Awanso amaphatikizidwa kudzina loti “Ambuye Yesu Kristu.” “Kristu” amatanthauza kuti “Odzodzedwa.”

Yesu panthawi ina anatchulidwapo kuti “Emmanueli,” kutanthauza akuti “Mulungu alinafe.” Yesu amkazitchula Yekha kuti “Mwana wa munthu” ndipo kawirikawiri amatchulidwa kuti “Mwana wa Mulungu” muzolemba za mu Chipingano Chatsopano. Yohane anamutcha kuti “Mau” ndi “Nkhonsa ya Mulungu.”

Palinso ma ina ambiri amene anaperekedwa kwa Yesu, monga ngati “Mkate wa moyo,” “Kuwala kwa dziko lapansi,” ndi ena ambiri. Ndandanda wamainawa waperekedwa mu phunziro la

sukulu ya Harvestime Institute, “*Ndondomeko za uzimu: Buku la Nkhondo ya Uzimu*”. Dzina linalirilonse limene linaperekedwa kwa Yesu ndilofunika kwambiri pofuna kumvetsetsa pazaudindo ndi utumiki wake.

MMENE MAINA AMABWERERA

Pali njira zitatu zimene anthu opambana amalandirira maina:

POBADWA:

Anthu ena amabadwa ndi dzina lopambana. Amabadwa ngati mfumu, mfumukazi, kapena mwana wamtsoholeri wamtundu waukulu. Kapena atha kubadwira m’banja lomwe limadziwika ndi chuma chochuluka kapena lamphamvu pa ndale. Amatengera dzina lawo kuchokera kwa makolo awo.

PAMENE ACHITA ZOPAMBANA:

Anthu ena amapanga dzina chifukwa achita zopambana pamoyo wawo. Amasanduka kukhala wolembe opambana, andale ndi atsogoleri.

KUCHITA KUPATSIDWA:

Anthu ena amalandira dzina chifukwa lachita kupatsidwa pa iwo. Amapatsidwa dzina lopambana ndi anthu ena. Mwachitsanzo, mzimayi wosauka amalandira dzina la munthu wandale wolemera pamene akwatirana. Mfumu kapena mtsogoleri wa mtundu amatha kupereka dzina kwa munthu wina mu ufumumo kapena kumtundu.

MMENE YESU ANALANDIRIRA DZINA LAKE

Yesu analandira dzina lake kupyolera munjira zonse zitatu zapadziko lapansi:

POBADWA:

Yesu analandira dzina Lake pobadwa, kupyolera kutengera kwa Atate Ake:

KALE Mulungu analankhula ndi makolo mwa aneneri m'manenedwe ambiri ndi mosiyana-siyana, koma pakutha pace pa masiku ano analankhula ndi ife ndi Mwana amene anamuika wolowa nyumba wa zonse, mwa Iyenso analenga maiko ndi am'mwamba omwe; ameneyo, pokhala ali cinyezimiro ca ulemerero wace, ndi cizindikilo ceni ceni ca cikhalidwe cace, nanyamula zonse ndi mau a mphamvu yace,

m'mene adacita ciyeretso ca zoipa, anakhala pa dzanja lamanja la Ukulu m'Mwamba, atakhala wakuposa angelo, monga momwe adalowa dzina lakuposa iwo. (Ahebri 1:1-4)

Yesu anatengera dzina lopambana kuposa wina aliyense padziko. Dzina lake ndilopambana kuposa mfumu, mtsogoleri wa dziko kapena mtsogoleri wa mtundu.

KUPYOLERA PA ZOMWE ANACHITA ZOPAMBANA:

Yesu analandiraso dzina Lake chifukwa anagonjetsa mphamvu zonse za mdani:

atabvula maukulu ndi maulamuliro, anawaonetsera poyera, nawagonjetsera nako. (Akolose 2:15)

KUCHITA KUPATSIDWA:

Yesu dzina lake anachita kupatsidwa:

Mwa icinso Mulungu anamkwezetsa iye, nampatsa dzina limene liposa maina onse, kuti m'dzina la Yesu bondo liri lonse lipinde, la za m'mwamba ndi za padziko, ndi za pansu pa dziko, ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Kristu ali Ambuye, kucitira ulemu Mulungu Atate. (Afilipi 2:9-11)

DZINA LOPAMBANA

Dzina la Yesu ndi dzina la mphamvu kwambiri mu dziko lonse. Liri pamwamba pamaina onse:

Mwa icinso Mulungu anamkwezetsa iye, nampatsa dzina limene liposa maina onse, (Afilipi 2:9)

pamwamba pa ukulu wonse, ndi ulamuliro ndi mphamvu, ndi ufumu, ndi dzina liri lonse lochedwa, si m'nyengo yinoya pansu pano yokha, komanso mwaiyo ikudza; (Aefeso 1:21)

MPHAMVU MU DZINA

Yesu anawasiyira otsatira Ake ntchito yaikulu yokafikira dziko lonse lapansi ndi Uthenga Wabwino. Anawasiyiraso mphamvu zapaderadera zoti zimawapangitse kuti akwakwaniritse ntchito imeneyi. Anawapatsa ulamuliro ogwiritsa ntchito dzina Lake:

Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi. Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a

mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano. (Mateyu 28:18-20)

Pamene munthu wapereka dzina lake kwa wina, zimatanthauza kuti awiriwo alumikizana pamodzi mugwirizano wapaderadera. Chitsanzo ndi Mulungu pamene anapereka dzina Lake kwa Israeli:

Yehova adzakukhazikirani yekha mtundu wa anthu wopatulika, monga anakulumbirirani; ngati mudzasunga malamulo a Yehova Mulungu wanu, ndi kuyenda m'njira zace. Ndipo anthu onse a pa dziko lapansi adzaona kuti akuchulani dzina la Yehova; nadzakuopani. (Deuteronomo 28:9-10)

Kutumizidwa kapena kukayankhula pa dzina la wina zikutanthauza kuti umatengaso ulamuliro wake:

Cifukwa cace atero Yehova za anthu a Anatoti, amene afuna moyo wanga, kuti, Usanenere m'dzina la Yehova, ungame ndi mkono wathu; cifukwa cace atero Yehova wa makamu, Taonani, ndidzalanga iwo; anyamata adzafa ndi lupanga; ana ao amuna ndi akazi adzafa ndi njala; (Yeremiya 11:21-22)

Anthu oipa anayesera kumupha Yeremiya chifukwa amkanenera mudzina la Ambuye ndipo amkadziwa kuti uneneri wake uli ndi ulamuliro wa Mulungu kuseli kwake.

Chifungulo chimodzi chofunikwa kwambiri ku mphamvu ya uzimu ndi dzina la Yesu. Nthawi zambiri timalephera muutumiki chifukwa timadalira kuthekera kwathu pofuna kumumasula wina. Sidzina lathu, udindo, kapena ulamuliro zomwe zimanyamula mphamvu. Mphamvu zanthu ziri mu dzina la Yesu.

Kumangokuwa chabe za dzinali mobwerezabwereza zimangosanduka chikhalidwe. Limasanduka kukhala lopanda ntchito mkuyamba kufa monga momwe amkachitira Afalisi ndi Alembi munthawi ya Baibulo. Dzina la Yesu limagwiritsidwa ntchito monga mmene achitira amatsenga. Mukuyenera kukhala ndi chikhulupiriro mu dzinalo. Ophunzira anatsindika ichi potsatira kuchiritsidwa kwa mphamvu komwe kunalembedwa pa Machitidwe 3. Petro anati:

Ndipo pa cikhulupiriro ca m'dzina lace dzina lacelo linalimbikitsa iye amene mumuona, nimumdziwa; ndipo cikhulupiriro ciri mwa iye cinampatsa kucira konse kumeneku pamaso pa inu nonse. (Machitidwe 3:16)

Tanenelera dzina la Yesu ngati asing'anga, koma cikhulupiriro chanthu mu dzinalo chakhala chofooka. Kodi tingaposere bwanji pongogwiritsa ntchito dzina la Yesu wamba mkuyamba kukhala ndi cikhulupiriro mu dzina lomwe limabweretsa mphamvu? Baibulo limati:

Comweco cikhulupiriro cidza ndi mbiri, ndi mbiri idza mwa mau a Kristu. (Aroma 10:17)

Chikhulupiriro chanu mu dzina la Yesu chikhoza kukula pakumva zomwe Mau a Mulungu akukamba zokhudzana ndi dzinalo

MUDZINA LA YESU

Dzina la Yesu limagwiritsidwa ntchipo...

PACHIPULUMUTSO:

Mphamvu yaikulu mu dzina la Yesu ndi mphamvu ya kupulumutsa ku tchimo. Ndikupyolera mu dzina Lake lokha mmene chipulumutso chimabwera:

Ndipo adzabala mwana wamwamuna, ndipo udzamucha dzina lace Yesu; pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ace ku macimo ao. (Mateyu 1:21)

Ndipo anamucha Bamaba, Zeu; ndi Paulo, Herme, cifukwa anali wotsogola kunena. (Machitidwe 4:12)

Wokhulupirira Iye saweruzidwa; wosakhulupira waweruzidwa ngakhale tsopano, cifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu. (Yohane 3:18)

Simungakhululukidwe machimo anu munjira iliyonse koma kupyolera mu dzina la Yesu lokha basi. Simungafike kwa Mulungu osadutsira mwa Yesu:

Yesu ananena naye, ine ndinenjira, ndi coonadi, ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine. (Yohane 14:6)

Pamene talalikira Uthenga Wabwino ndi kofunika kwambiri kuti tizitsindike kuti chipulumutso chimabwera kuchokera mudzina la Yesu yekha basi. Kuvomereza dzina la Yesu ndi kofunika pachipulumutso:

kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka: pakuti ndi mtima munthu akhulupira kutengapo cilungamo; ndi m'kamwa abvomereza kutengapo cipulumutso (Aroma 10:9-10)

Mphamvu yokhala mwana wa Mulungu imabwera kupyolera mudzina la Yesu:

Koma onse amene anamlandira iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lace; (Yohane 1:12)

KUYERETSA:

simumangosambitsidwa kokha ku tchimo ndi kulungamitsidwa kudzera mu dzina la Yesu, komaso mumayeretsedwa. Kuyeretsedwa kumabwera kupyolera mu mphamvu ya Mulungu imene imapitiriza kugwirabe ntchito mwainu potsatira chipulumutso Pa Akorinto 6, Paulo akuyakhula zoipa za uchimo.

Iye anati:

Ndipo ena ainu munali otere; koma munasambitsidwa, koma munayeretsedwa, koma munayesedwa olungama, m'dzina la Ambuye Yesu Kristu, ndi mwa Mzimu wa Mulungu wathu. (1 Akorinto 6:11)

Mbuyomu, Akorinto amenewa amkakhala machitidwe auchimo. Koma tsopano anayamba kukhala moyo wachiyero kudzera mkuyeretsedwa komwe kunabwera mudzina la Yesu.

MUPEPHERO:

Kufikira tsopano simunapempha kanthu m'dzina langa; pemphani, ndipo mudzalandira, kuti cimwemwe canu cikwaniridwe. (Yohane 16:24)

Kufikira pa nthawi imene Yesu amkayakhula mau amenewa, mkuti ophunzira Ake asanapepheko kalikonse mu dzina Lake. Pa nthawi iyi anakhazikitsa ubale watsopano ndi iwo. Anawauza kuti azimupepha Mulungu china chirichonse mu dzina Lake:

Ndipo tsiku limenelo simudzandifunsa kanthu. Indetu, indetu, ndinena kwa inu, Ngati mudzapempha Atate kanthu, adzakupatsani inu m'dzina langa. (Yohane 16:23)

Lonjezo lotani la mphamvu iri! China chirichose tingapephe mu dzina Lake, tizalandira.

Koma lonjezano limeneri likuyenera kuyenda limodzi ndi ndondomeko zina za pephero zomwe zanenedwa m'Baibulo. Sitingasiye vesi ina pambali pa phunziro popanda kuyang'ana zonse zimene zanenedwa muphunziroli mu Mau a Mulungu. Baibulo limaphunzitsa kuti simungapephe mozikonda:

Mupempha, ndipo simulandira, popeza mupempha koipa, kuti mukacimwaze pocita zikhumbitso zanu. (Yakobo 4:3)

Mukuyeneraso kumakhala mwachiyero pamaso pa Mulungu. Ngati muchimwa, mukuyenera kuvomereza ndi kupepha chikhululukiro:

Cifukwa cace mubvomerezane wina ndi mnzace macimo anu, ndipo mupempherere wina kwa mnzace kuti muciritsidwe. Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukuru m'macitidweace. (Yakobo 5:16)

Simungapitirire kukhalabe mu uchimo ndi kumaganiza kuti chifukwa mwapepha mu dzina la Yesu ndiye kuti muzalandira zopepha zanu. Ndi pephero la amuna ndi akazi olungama lomwe limapambana ndi Mulungu:

Ngati mukhala mwa Ine, ndi mau anga akhala mwa inu, pemphani cimene ciri conse mucifuna ndipo cidzaciditika kwa inu. (Yohane 15:7)

Izi zikuthanthauza kuti ngati mukukhalabe mwa Kristu mutha kupepha china chirichonse ndipo chizapatsidwa. Ngati mukuyenda mukumvera Mulungu, mutha kupepha mu dzina la Yesu.

Kupephera mu dzina la Yesu zimakhalaso ku chifuniro cha Mulungu. Yesu anapephera:

Nati, Atate, mukafuna Inu, cotsani cikho ici pa Ine; koma si kufuna kwanga ai, komatu kwanu kucitike. (Luka 22:42)

Pazifooko za thupi la munthu, Yesu sanafune kuti akazuzike. Amkafuna kuti chikho chamazuzo chimpitirire, koma anapereka chifuniro chake kuchifuniro cha Mulungu.

Muzochitika zina zomwe zinalembedwa mmalemba momveka bwino,timadziwa kuti ndi chifuniro cha Mulungu chimene tingapepherere. Muzochitika zina titha kuonetsera chifuniro chanthu. Monga mmene Yesu anachitira, kenako mkupereka chifuniro chathu ku chifuniro Chake kudzera mudzina la Yesu.

Pempho loperekedwa mu dzina la Yesu limagonjera chifuniro cha Munthu wamphamvu. Timapempha malingana ndi malingaliro a umunthu ndipo nthawi zonse sitimazindikira chifuniro chachikulu cha Mulungu:

Pakuti maganizo anga sali maganizo anu, ngakhale njira zanu siziri njira zanga, ati Yehova. Pakuti monga kumwamba kuli kutari ndi dziko lapansi, momwemo njira zanga ziri zazitari kupambana njira zanu, ndi maganizo anga kupambana maganizo anu. (Yesaya 55:8-9)

Nthawi zonse simungadziwe chifuniro cha Mulungu malingana ndi mmene mungapepherere. Pamene simukutsimikizika pa chifuniro cha Mulungu, ndikwabwino kupemphera ndi chilakhulo cha Mzimu Woyera. Mzimu Woyera amapembedzera mwalo mwanthu mogwirizana ndi chifuniro cha Mulungu:

Ndipo anawapatsa copempha iwo; Koma anaondetsa mitima yao. (Salimo 106:15)

Ena atha kusagwirizana ndi chiphunzitso cha Baibulo. Atha kumati simungapemphe kalikonse mu dzina la Yesu ndikupatsidwa. Ngati mupemphera mwamwano popanda kupereka zopempha zanu ku chifuniro cha Mulungu, Atha kuyakha zopempha zanu, koma osati mokukomerani inu. Anachita izi ku fuko la Israeli:

Ndipo anawapatsa copempha iwo; Koma anaondetsa mitima yao. (Salimo 106:15)

Palibe yemwe, kupyolera mukupemphera mu dzina la Yesu, angakakhe china chake kwa munthu wina chimene munthu ameneyu sakuchifuna. Mulungu samachotsa chifuniro cha munthu. Chifuniro cha munthu wina ndi kusakhulupira zikhoza kukhudza mapemphero anu kwa iwo. Yesu anayakhula za mphamvu pakumvomerezana ndi ena mukupephera mu dzina la Yesu:

Ndiponso ndinena kwa inu kuti ngati awiri ainu abvomerezana pansu pano cinthu ciri conse akacipempha, Atate wanga wa Kumwamba adzawacitira. Pakuti kumene kuli awiri kapena atatu asonkhanira m'dzina langa, ndiri komweko pakati pao. (Mateyu 18:19-20)

Ngati mbali imodzi ya pephero, kuthokoza kukuyenera kuperekedwa mu dzina la Yesu:

ndi kuyamika Mulungu Atate masiku onse, cifukwa ca zonse, m'dzina la Ambuye wathu Yesu Kristu; (Aefeso 5:20)

Mukuyeneraso kuthokoza mu dzina la Yesu:

Potero mwa iye tipereke ciperekere nsembe yakuyamika Mulungu, ndiyo cipatso ca milomo yobvomereza dzina lace. (Ahebri 13:15)

Muphunzira zambiri zokhudzana mphamvu ya pephero mu chaputala chotsatira.

MBALI ZONSE ZAUTUMIKI:

Dzina la Yesu likuyenera kugwiritsidwa ntchito mbali zonse za utumiki:

Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi. Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansu pano. (Mateyu 28:18-20)

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Marko 16:17-18)

Malingana ndi ma vesi amenewa, mautumiki otsatirawa akuyenera kuchitika mu dzina la Yesu:

Zizindikiro ndi zozizwa:

Zizindikiro ndi zozizwa zonse zikuyenera kuchitidwa mu dzina la Yesu. Ophunzira anapepera:

Ndipo tsopano Ambuye, penyani mau ao akuopsa, ndipo patsani kwa akapolo anu alankhule mau anu ndi kulimbika mtima konse, m'mene mutambasula dzanja lanu kukaciritsa; ndi kuti zizindikilo ndi zozizwa zicitidwe mwa dzina la Mwana wanu wopatulika Yesu. (Machitidwe 4:29-30)

Kulalikira ndikuphunzitsa:

Yesu anati mphamvu zonse ndi ulamuliro zapatsidwa kwa Iye ndipo kupyolera mu mphamvu yotumidwa kukalalika ndi kukaphunzitsa za Uthenga Wabwino mu dzina la Yesu.

Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano. (Mateyu 28:19-20)

ndipo anati kwa iwo, 8 Koteru kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lacinatu; ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi 9 kukhululukidwa kwa macimo kwa 10 mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu. (Luka 24:46-47)

Chifukwa chakuti anazindikira mphamvu mu dzina la Yesu, adani a Uthenga Wabwino anawachenjeza ophunzira kuti:

Komatu tiwaopse asalankhulenso m'dzina ili kwa munthu ali yense, kuti cisabukenso kwa anthu. Ndipo anawaitana, nawalamulira kuti asanene konse kapena kuphunzitsa m'dzina la Yesu. (Machitidwe 4:17-18)

Koma Petro anayakha kuti:

pakuti sitingatheife kuleka kulankhula zimene tinazona ndi kuzimva. (Machitidwe 4:20)

Ophunzira anachitira umboni mphamvu ya Mulungu. Zinthu zomwe anawona ndi kumva mu dzina la Yesu zinali ndi mphamvu imene inawapangitsa kuti apite kukakwaniritsa mautumiki awo.

Simukuyenera kungophunzitsa kokha mu dzina la yesu, mukuyenera kukaphunzitsanso dzinalo:

Koma pamene anakhulupirira Filipino wakulalikira Uthenga Wabwinowa Ufumu wa Mulungu ndi dzina la Yesu Kristu, anabatizidwa, amuna ndi akazi. (Machitidwe 8:12)

Ubatizo:

Otembenuka mtima atsopano akuyenera kubatizidwa mmadzi mu dzina la Atate, la Mwana Yesu, ndi la Mzimu Woyera:

Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: (Mateyu 28:19)

Pamene anamva ici, anabatizidwa m'dzina la Ambuye Yesu. (Machitidwe 19:5)

Pa dzina limeneri, okhulupirira analandira mphatso ya Mzimu Woyera:

Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. (Machitidwe 2:38)

Kutulutsa ziwanda:

Ziwanda ndi angelo a satana. Poyambapo anali angelo a Mulungu amena analowa gulu la satana pomuukira Mulungu. Pano ali gawo limodzi ya satana imene ikugwira ntchito pa dziko lapansi munjira zambiri zoipa.

Ziwanda zimalowa osakhulupirira ndipo zimayamba kuwagwiritsa ntchito. Mphamvu za ziwanda zimatha kumazuka okulupirira, koma sizingawalowe. Mphamvu zawo za usatana zikuyenera kuphwasulidwa mu dzina la Yesu:

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano;Marko 16:17)

Pamene Paulo anafikiridwa ndi mzimayi waziwanda, anati:

Ndipo anacita coteri masiku ambiri. Koma Paulo anabvutika mtima ndithu, naceuka, nati kwa mzimuwo, Ndikulamulira iwe m'dzina la Yesu Kristu, turuka mwa iye. Ndipo unaturuka nthawi yomweyo. (Machitidwe 16:18)

Chiphunzitso chatsatane tsatane chokhudzana ndi ziwanda ndi momwe mamasulidwe angabwerere kwa onse amene ali panso pa mphamvu yawo ndi machitichita awo zaperekedwa mu phunziro la sukulu ya Harvestime International Institute, *“Ndonomeko za uzimu: Buku la Nkhondo ya Uzimu.”*

KUTUMIKIRA MU MZIMU WOYERA:

Mzimu Woyera anaperekedwa mu dzina la Yesu:

Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa, 3 Iyeyo adzaphunzitsa Inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu. (Yohane 14:26)

Kuyakhula malilime atsopano kupyolera mwa Mzimu zinagwiritsidwa ngati chitsanzo chama utumiki Ake osiyanasiyana mu vesi limeneli:

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; (Marko 16:17)

Mphatso zonse za Mzimu Woyera zikuyenera kugwiritsidwa ntchito mu dzina la Yesu. Mphatso ya malilime ndi imodzi ya mphatso za uzimu. Mphatsoyi yagwiritsidwa ntchito yoimirira ma utumiki onse a Mzimu Woyera popeza ndi imene inali yoyamba kulandiridwa pamene Mzimu Woyera anaperekedwa.

KUCHILITSA:

Dzina la Yesu liyenera kugwiritsidwa ntchito mu utumiki wochiritsa kwa onse amene akudwala:

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Marko 16:17-18)

Pali wina kodi adwala mwa inu? Adziitanire akuru a Mpingo, ndipo apemphere pa iye, atamdzoza ndi mafuta m'dzina la Ambuye: (Yakobo 5:14)

Pamene Yesu anafa pamtanda, anazuzika osati chifukwa chamachino anu okha koma kuti abweretse machiritso anu:

Taona, iwe udzaitana mtundu umene sunaudziwa, ndi mtundu umene sunakudziwa udzakuthamangira, cifukwa ca Yehova Mulungu wako, ndi cifukwa ca Woyera wa Israyeli; pakuti Iye wakukometsa. (Yesaya 53:5)

kotero kuti cikwaniridwe conenedwa ndi Yesaya mneneri, kuti, Iye yekha anatenga zofoka zathu, Nanyamula nthenda zathu. (Mateyu 8:17)

**amene anasenza macimo athu mwini yekha m'thupi mwace pamtanda, kuti ife, 7
titafa kumacimo, tikakhale ndi moyo kutsata cilungamo; 8 ameneyo
mikwingwirima yace munaciritsidwa nayo. (1 Petro 2:24)**

Kodi kumakhala kophweka bwanji kulandila chipulumutso cha tchimo kupyolera mu dzina Lake, kodi zimakhala zolimba kwaife kukhulupirira machilitso kupyolera mu dzina Lake?

Pamene ophunzira anakumana ndi munthu wolumala pa khomo la Kachisi, Petro anati:

**Ndipo pa cikhulupiriro ca m'dzina lace dzina laceo linalimbikitsa iye amene
mumuona, nimumdziwa; ndipo cikhulupiriro ciri mwa iye cinampatsa kucira konse
kumeneku pamaso pa inu nonse. (Machitidwe 3:6)**

Petro anazindikira mphamvu imene inali mu dzina la Yesu. Anazindikira kuti muli machiritso mu dzina la Yesu. Anazindikira kuti anali ndi ulamuliro ogwiritsa ntchito dzina limeneri “Monga zomwe ndiri nazo!” Mphamvu zimene zinali kumbuyo kwa dzina limeneri zinaperekedwa kwa iye ndi Yesu.

Ndalama ndi zofunika mu ntchito ya utumji, koma kusowa kwa thandizo sikungaimitse utumiki wowona wa mphamvu ya Mulungu. Petro ndi Yohane analibe Siliva kapena Golide, koma anapitirizabe kutumikira mphamvu kupyolera mu dzina la Yesu.

Amuna awa analibe ndalama zoti alengezere utumiki wawo mu mzinda wa Yerusalemu. Koma mzinda onse unazindikira za izi kupyolera mukuwonetsera mphamvu ya Mulungu. Mukhoza kuwerenga za izi pa Machitidwe 3 ndi 4.

PA CHITETEZO:

**Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa
ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo
ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa
odwala, ndipo adzacira. (Marko 16:17-18)**

Mtumwi Paulo analumidwa ndi njoka ya ululu kwambiri koma sinamuvulaze. Mukhoza kuwerenga za izi pa Machitidwe 28

MUZINTHU ZONSE:

Baibulo limati china chirinse tichita tichite mudzina la Yesu:

Ndipo ciri conse mukacicita m'mau kapena muncbito, citani zonse m'dzina la Ambuye Yesu, ndi kuyamika Mulungu Atate mwa iye. (Akolose 3:17)

Pamene muchita chinachirichonse mu dzina la Yesu, ngakhale pa zinthu zazing'ono zimasanduka kukhala zamphamvu mu uzimu. Mutha kumasesa mu Tchalitchi mu dzina la Yesu. Mutha kumakoza chakudya chabanja lanu mudzina la Yesu. Zomwe mukuchita sizofunika koma mmene mukuchitira. Kodi zimachitika mudzina la Yesu?

KUZUZIDWA CHIFUKWA CHADZINA

Kumbukilani mau amene Ine ndinanena kwa inu, Kapolo sali wamkuru ndi mbuye wace. Ngati anandilondalonda Ine, adzakulonda-londani inunso; ngati anasunga mau anga, adzasunga anunso. Koma izi zonse adzakucitirani cifukwa ca dzina langa, cifukwa sadziwa wondituma Ine. (Yohane 15:20-21)

Pamena ophunzira anazuzidwa chifukwa cha Uthenga Wabwino:

Sindikadacita mwa iwo nchito zosacita wina, sakadakhala nalo cimo; koma tsopano anaona, nada: Ine ndi Atate wanganso, Koma citero, kuti mau olembedwa m'cilamulo cao akwaniridwe, kuti, Anandida Ine kopanda cifukwa. (Machitidwe 15:24-25)

Ngakhale Yesu analonjeza chitetezo pamene mwalowa muutumiki, izi sizikutathauza kuti ophunzira sanazuzidwe. Petro, Paulo ndi Sila anaikidwa ndende. Ophunzira amenewa anagendedwa ndiposo kukwapulidwa, ndipo Paulo nthawi ina anasiyidwa ndi adani a Uthenga Wabwino atatsala pang'ono kufa. Pamena mautumiki awo amapita kumapeto, ambiri mwa ophunzirawa imfa zawo zinali zochita kuphedwa chifukwa cha Uthenga Wabwino. Petro yemwe analanditsidwa ku ndende patsogolo pake anaphedwa chifukwa cha Uthenga Wabwino, Ahebri 11 imakamba nkhani ya amuna ndi akazi opambana amene anatumikira kupyolera mchikhulupiriro. Koma mafotokozanso nkhani ya onse amene anafa mchikhulupiriro chifukwa cha Uthenga Wabwino pamene mautumiki awo anatha, Petro anafotokoza kuti:

Mukatonzedwa pa dzina la Kristu, odala inu; pakuti Mzimu wa ulemerero, ndi Mzimu wa Mulungu apuma pa inu. (1 Petro 4:14)

Muphunzira zambiri zokhudzana mphamvu yachiyanjano mazuzo Ake mu chaputala 17.

KULAMULIRA CHIFUKWA CHA DZINA

Kupyolera mu dzina la Yesu, mumakhala mbali imodzi ya ufumu wa Mulungu:

ndi kuyamika Atate, amene anatiyeneretsa ife kulandirana nao colowa ca oyera mtima m'kuunika; amene anatilanditsa ife ku ulamuliro wa mdima, natisunthitsa kutilowetsa m'ufumu wa Mwana wa cikondi cace; (Akolose 1:12-13)

Monga ngati mbali imodzi ya ufumu wa Yesu, mumalandira cholowa cha mphamvu cholamulira mmoyo.

Pakuti ngati, ndi kulakwa kwa mmodzi, imfa inacita ufumu mwa mmodziyo; makamaka ndithu amene akulandira kucuruka kwace kwa cisomo ndi kwa mphatso ya cilungamo, adzacita ufumu m'moyo mwa mmodzi, ndiye Yesu Kristu. (Aroma 5:17)

Mukuyenera kulamulira moyo kudzera mu dzina la Yesu. Mukuyenerea kulamulira mphamvu zonse za mdaniyo kupyolera mu dzina la Yesu.

UMBONI WOMALIZA

Umboni womaliza wa Baibulo pa dzina la Yesu ukupezeka mu buku la Chibvumbulutso. Limayakhula za tsiku limene okhulupirira azakhale pamaso pa mpulumutsi wawo kudziko lakumwamba ndi lapansi latsopano.

(Chibvumbulutso 22:3-4)

- Dzina limene timakondwera nalo...
- Dzina limene tagwiritsa ntchito mwa ulamuliro ndi lomwe tapephelera...
- Dzina limene timalamulira nalo mmoyo...
- DZINA LA YESU...lizakhala mbali imodzi ya chizindikira chanthu kuumuyaya onse.

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Fotokozani kufinika kwa maina mu nthawi ya Baibulo.

3. Ndi ndani amene anamulamula Yosefe kuti ampatse dzina Yesu?

4. Kodi dzina lalikulu pa dziko lonse ndiriti?

5. Kodi Yesu anatenga bwanji dzina Lake?

6. Kodi mungakhazikitse bwanji chikhulupiriro chanu mu dzina la Yesu ndi mphamvu Yake?

7. Werengani ndime zotsatirazi ndipo muike mau amene akusowa mumpatamo kuti mumalizitse mawuwo.
 - a. Dzina la Yesu ndirofunika chifukwa_____.
 - b. Pamene tikupephera wo_____wodwala, likuyenera kukhala mu dzina la Yesu.
 - c. Chi_____chimabwera kupyolera mu dzina la Yesu.
 - d. Tikuyenera ku_____ndiku_____mudzina la Yesu.
 - e. Kutulutsa ziw_____kukuyenera kuchitika mu dzina la Yesu.
 - f. Tikuyenera ku_____mudzina la Atate, la Mwana, ndi la Mzimu Woyera.
8. Lembani kuti ZOWONA kapena ZONAMA pampata patsogolo pa ndime iriyonse.
 - a. _____tikuyenerera kupereka chiyamiko muchina chirichonse ku dzina la Yesu.
 - b. _____Mzimu Woyera anaperekedwa mu dzina la Yesu.
 - c. _____chitetezo mu dzina la Yesu chimatanthauza kuti sitikuyenera kuzuzika chifukwa cha Iye.

(Mayankho amayesowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Pitirizani kuwerenga paza mphamvu mu dzina la Yesu pogwiritsa ntchito ndandandawu.

Mateyu: 1:21; 1:23; 1:24,25; 10:22; 12:18,21; 18:5; 18:19,20; 19:29; 28:19

Marko: 9:38-41; 16:17-18

Luka: 10:17; 24:46-47

Yohane: 1:12; 2:23; 3:18; 14:13-14; 14:26; 15:16; 15:20-21; 16:23, 24, 26; 20:31

Machitidwe: 2:21; 2:38; 3:6; 3:16; 4:7,8,10,12,17,18; 4:29-30; 5:28,40-42; 8:12; 9:14-16; 9:21,27,29; 10:43; 10:48; 15:25-26; 16:18; 19:5

Aroma: 1:5; 10:13

1 Akorinto: 1:2; 1:10; 6:11

Aefeso: 5:20

Afilipi: 2:9-11

Akolose: 3:17

2 Atesalonika: 1:12

2 Timoteo: 2:19

Ahebri: 1:4; 6:10; 13:15

Yakobo: 5:14

1 Petro: 4:14

1 Yohane: 2:12; 3:23; 5:13

Chibvumbulutso: 19:12, 13, 16; 22:3-4

CHAPUTALA 13

NDONDOMEKO YA MPHAMVU 7:

MPHAMVU YAPEMPHERO

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osawonera.
- Kufotokoza mmene pemphero ndi kusala kudyā kumamasulira mphamvu ya Mulungu.
- Kupereka tanthauzo la pemphero.
- Kufotokoza mlingo osiyanasiyana wa pemphero.
- Kufotokoza mitundu yosiyanasiyana ya pemphero.
- Kupereka tanthauzo lakusala kudyā.
- Kupereka mitundu iwiri ya kusala kudyā.
- Kufotokoza cholinga chakusala kudyā.

VESI YOTSOGOLERA:

Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukuru m' mschitidwe ake.(Yakobo 5:16b).

MAU OYAMBA

Monga momwe mwaphunzirira zokhudzana ndi mphamvu mu dzina la Yesu mwaphunzira kuti okhulupirira akhoza kugwiritsa ntchito dzina Lake mu pemphero pofuna kupereka zopezha kwa Atate. Phunziro ili likufufuza mphamvu ya pemphero mu dzina la Yesu. Komaso tifotokozera kusakaniza pemphero ndi kusala kudyā. Kupemphera ndikusala kudyā ndi ndondomeko ya mphamvu kwambiri imene imamasula mphamvu ya Mulungu miyoyo ya okhulupirira.

TANTHAUZO LA PEMPHERO

Pemphero ndi kuyanjana ndi Mulungu. Limachitika mosiyana-siyana, koma kwakukuru ndi pamene munthu alankhula ndi Mulungu ndi Mulungu alankhula ndi munthu. Pemphero lafotokozeredwa ngati:¹

- Kuitanira pa dzina la Mulungu Genesis 12:8
- Kulirira kwa Mulungu Masalimo 27:7; 34:6
- Kuyandikira kwa Mulungu Masalimo 73:28; Aheberi 10:22
- Kuyang'ana kumwamba Masalimo 5:3
- Kukweza moyo Masalimo 25:1
- Kukweza mtima Maliro 3:41
- Kukhuthula mtima Masalimo 62:8
- Kukhuthula moyo 1 Samuel 1:15
- Kulirira kumwamba 2 Mbiri 32:20
- Kudandaulira Ambuye Eksodo 32:11
- Kufunafuna Mulungu Yobu 8:5
- Kufunafuna nkhope ya Ambuye Masalimo 27:8
- Kupemphelera Yobu 8:5; Yeremiya 36:7

MOYO WA PEMPHERO WA YESU

Pemphero inali njira yodalirika kwa Ambuye Yesu:

YESU ANAIKA PEMPHERO PATSOGOLO:

¹*Zophunziridwa zina mu chaputala chino zatengedwa mu chaputala cha pemphero ndikusala kudya mu “*Ndodomeko za Uzimuz: Buku la Nkhondo ya uzimu.*” Pachifukwa chimenechi zophunzira zabwerezedwaso pamene zophunzira zotsapano zaperekedwaso.

- Amapemphera nthawi iliyonse masana kapena usiku: Luka 6:12-13
- Pemphero linali patsogolo osati kudya Yohane 4:31-32
- Pemphero linali patsogolo osati utumiki: Yohane 4:31-32

PEMPHERO LIMAPEZEKEZA PA CHOCHITIKA CHILICHONSE CHOFUNIKA:

- Pamene amabatizidwa Luka 3:21-22
- Ulendo wake woyamba wa utumiki Marko 1:35; Luka 5:16
- Asanasankhe ophunzira Luka 6:12-13
- Asanadyetse komanso atamaliza kudiyetsa anthu zikwi zisanu: Mateyu 14:19, 23; Marko 6:41, 46; Yohane 6:11, 14-5
- Podyetsa anthu zikwi zinayi Mateyu 15:36; Marko 8:6, 7
- Petro anabvomereza Luka 9:18
- Yesu anasandulike pa phiri Luka 9:18, 29
- Pakubwerera kwa makumi asanu ndi awiriwo Mateyu 11:25; Luka 10:21
- Pa manda a Lazaro Yohane 11:41-42
- Pakudalitsa ana Mateyu 19:13
- Pakubwera kwa Aheleni ena Yohane 12:27-28
- Lisanafike ola la msautso wake Mateyu 26:26-27; Marko 14:22-23; Luka 22:17-19
- Kupemphelera Petro: Luka 22:32
- Kuti Mzimu Woyera aperekedwe: Yohane 14:1-6
- Pa njira ya ku Emmau: Luka 24:30-31
- Asanakwere kunka kumwamba: Luka 24:50-53
- Kupempherera omutsatira ake: Yohane 17
- Pemphero lomwe Yesu anaphunzitsa liri pa Mateyu 6:9-13.

Paulo akupempha ophunzira kuti apemphere nthawi zonse ndi “mapemphero onse” (Aefeso 6:18). Pena analemba kuti “kupemphera ndi mtundu uliwonse wa pemphero.” Izi zikutanthauza kuti pali milingo ndi mitundu yosiyana-siyana ya pemphero.

MILINGO YA PEMPHERO

Pali milingo itatu yopemphera mosweka mtima: kupempha, kufunafuna, kugogoda.

Pemphani, ndipo cidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo cidzatsegulidwa kwa inu; pakuti yense wakupempha alandira; ndi wakufunayo apeza; ndi kwa wogogodayo citseguldwa. (Mateyu 7:7-8).

Kupempha ndi mulingo woyamba wa pemphero. Ndiko kupereka chabe chopempha kwa Mulungu kulandira mayankho mwamsanga. Kutu munthu alandire akuyenera kupempha:

.... mulibe, chifukwa simupempha (Yakobo 4:2).

Pemphero ndi chida chazimu champhamvu kwambiri, koma ambiri sachigwiritsa ntchito. Sapempha, chifukwa cha ichi salandira kanthu.

Kufunafuna ndi mlingo wina wozamirapo pang’ono. Uwu ndi mlingo umene mayankho sabwera mwamsanga ngati m’mlingo woyamba uja wa kupempha. Okhulupirira zana limodzi ndi makumi awiri omwe anali m’chipinda chapamwamba “anapitirira” m’pemphero ndipo ichi ndi chiitsanzo cha kufuna-funa. Amuna ndi akazi awa anakhumba kukwaniritsidwa kwa lonjezani la Mzimu Woyera ndipo anapitirira “kufuna-funa” mpaka yankho linafika (Machitidwe 1-2).

Kugogonda ndi mlingo wozama kwambiri. Ili ndi pemphero lomwe munthu amalimbikabe ndipo mayankho amatenga nthawi kuti abwere. Izi zafotokozeredwa bwino mu fanizo lomwe Yesu anapereka mu Luka 11:5-10. Mlingo wogogoda ndi mulingo wovuta kwambiri pomenya nkhondo yauzimu m’pemphero. Tikhoza kumvetsa bwino za mulingo wa kugogoda tikaona nkhani ya Daniel amene analimbikabe kugogoda posatengera kuti sanaone chizindikiro chirichonse chakuti Mulungu wamuyankha. Satana atatchinga mayankho ake ochokera kwa Mulungu (Daniel 10).

MITUNDU YA PEMPHERO

Pali mitundu yosiyana-siyana ya pemphero yomwe timaipeza mu pemphero la Ambuye lomwe liri ngati mlozo wathu wa pemphero (Mateyu 6:9-13).

1. **KULAMBIRA NDI MATAMANDO:**

Timayenera kufika pamaso pa Mulungu ndi kulambira pamodzi ndi kukweza:

**Lowani ku zipata zace ndi ciyamiko, Ndi ku mabwalo ace ndi cilemekezo:
Myamikeni; lilemekezeni dzina lace. (Masalimo 100:4).**

Kulambira ndi kupereka ulemu. Kutamanda ndiko kupereka chithokozo poonetsera kuyamika kwa Mulungu pa zomwe watichitira komanso chifukwa cha chimene Iye ali. Mukuyenera kupembedza Mulungu mu mzimu ndi m'choonadi:

(Yohane 4:23-24).

Malambiro ndi matamando atha kuchitika ndi:

- Kuyimba: Masalimo 9:2,11; 40:3; Marko 14:26
- Matamando omveka: Masalimo 103:1
- Kukuwa: Masalimo 47:1
- Kukweza manja kumwamba: Masalimo 63:4; 134:2; 1 Timoteyo 2:8
- Kuomba m'manja: Masalimo 47:1
- Zida zoyimbira: Masalimo 150:3-5
- Kuimilira: 2 Mbiri 20:19
- Kuwerama: Masalimo 95:6
- Kuvina: Masalimo 149:3
- Kugwanda: Masalimo 95:6
- Kugona pansu: Masalimo 149:5

Womanya nkhondo wa Mulungu mdziko lauzimu amaonekera ndi...

...matamando okweza a Mulungu... mkamwa mwao, ndi lupanga lakuthwa konse konse m'dzanja lawo (Masalimo 149:6).

2. **KUDZIPEREKA**

Ili ndi pemphero lopereka moyo ndi chifuniro chako kwa Mulungu. Limaphatikizapo pemphero la kudzipereka ndi kudziyeretsa.

3. **KUPEMPHA**

Ili ndi pemphero lopempha. Zopempha zikuyenera kuperekedwa kwa Mulungu molingana ndi chifuniro chake chomwe chabvumbulutsidwa m'Mau ake. Zopempha zitha kukhala pa milingo ya kupempha, kufuna-funa kapena kugogoda.

4. **KUBVOMEREZA NDI KULAPA**

Pemphero lobvomereza ndilo lolapa ndi kupempha chikhululukiro cha tchimo.

Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. (1 Yohane 1:9).

5. **KUPEMBEDZERA**

Ili ndi pemphero lopempherera ena. Wopembedzera ndi munthu amene amaima pamaso pa Mulungu m'malo mwa munthu wina kupempha ndi kudandaulira mavuto ake. Baibulo limanena kuti nthawi ina Mulungu anayang'ana pa dziko lapansi ndipo anaona kuti palibe aliyense yemwe akupembedzera:

Ndipo Iye anaona kuti palibe munthu, nazizwa kuti palibe wopembedzera; cifukwa cace mkono wace wace unadzitengera yekha cipulumutso; ndi cilungamo cace cinamcirikiza. (Yesaya 59:16).

Mulungu ataona kuti palibe wopembedzera, anatumiza Yesu:

Pakuti pali Mulungu mmodzi, ndi Mtetezi mmodzi pakati pa Mulungu ndi anthu, ndiye munthu, Kristu Yesu, (1 Timoteyo 2:5).

ndani adzawatsutsa? Kristu Yesu ndiye amene adafera, inde makamaka, ndiye amene adauka kwa akufa, amene akhalanso pa dzanja lamanja la Mulungu, amenenso atipempherera ife. (Aroma 8:34).

kucokera komwekoakhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa iye, popeza ali nao moyo wace cikhalire wa kuwapembedzera iwo. (Aheberi 7:25)

Tiana tanga, izi ndikulemberani, kuti musacimwe. Ndipo akacimwa wina, Nkhoswe tiri naye kwa Atate, ndiye Yesu Kristu wolungama; (1 Yohane 2:1)

M'bwalo la milandu mumakhala woimilira munthu amene akuimbidwa mulandu, kumulankhulira nkhani yake. M'nkondo yauzimu, kupembedzera ndi pemphero lopita kwa Mulungu m'malo mwa munthu wina.

Nthawi zina kupembedzera kumachitika ndi chidziwitso. Umapembedzera mu chilankhula chanu:

Ndidandaulira tsono, poyambayamba, kuti acitike mapembedzo, mapemphero, mapembedzero, mayamiko, cifukwa ca anthu onse; cifukwa ca mafumu ndi onse akucita ulamuliro kuti m'moyo mwathu tikakhale odika mtima, ndi acete m'kulemekeza Mulungu, ndi m'kulemekezeka monse. (1 Timoteyo 2:1-2).

Koma nthawi zina kumachitika ndi Mzimu Woyera. Kutha kuchitika ndi kubuula komwe kumabwera chifukwa cha katundu wauzimu wolemera kwambiri. Kutha kuchitika m'malilime osadziwika. Utha kumapembedzera munthu wina kapena Mzimu Woyera kupembedzera iweyo. Zikachitika izi, Mzimu Woyera kudzera mwa inu amalankhula kwa Mulungu molingana ndi chifuniro chake:

Ndipo momwemonso Mzimu athandiza kufoka kwathu; pakuti cimene tizipempha monga ciyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwiniatipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka; (Aroma 8:26)

Uwu ndi mlingo wozama kwambiri wa pemphero lopembedzera ndipo ndi wamphamvu koposa nkondo yauzimu.

MLOZO WA PEMPHERO

Nthawi ina Yesu analandira pempho lochititsa chidwi kuchokera kwa ophunzira ake:

...m'modzi mwa ophunzira ake anati kwa Iye, Ambuye, tiphunzitseni ife kupemphera... (Luka 11:1).

Ophunzirawa sanapemphe za kulalikira kapena kuchita zozizwa. Sanapemphe kuti aphunzire za kumanga maubwenzi okhazikika. Sanapemphe zodabwitsa kolandira machiritso a kuthupi.

Anapempha kuti aphunzitsidwe kupemphera.

- Pempherani nthawi zonse: Luka 21:36; Aefeso 6:18
- Pemphero mowirikiza: Aroma 12:12
- Pempherani kosalekeza: 1 Atesalonika 5:17
- Pempherani kwa Atate mu dzina la Yesu: Yohane 15:16
- Pempherani ndi kuyang'anira: 1 Petro 4:7
- Pempherani molingana ndi mlozo wa pemphero: Mateyu 6:9-13
- Pempherani ndi mtima wokhululuka: Marko 11:25
- Pempherani ndi kudzichepetsa konse: Mateyu 6:7
- Nthawi zina pemphero lichitike pamodzi ndi kusala kudya: Mateyu 17:21
- Pempherani mosweka mtima: Yakobo 5:16; Akolose 4:12
- Pempherani ndi kugonjera kwa Mulungu: Luka 22:42
- Gwiritsani ntchito njira yomanga ndi yomasula m'pemphero: Mateyu 16:19

ZOMWE MUNGAPEMPHERERE

- Mtendere wa Yerusalemu: Masalimo 122:6
- Ogwira ntchito m'munda: Mateyu 9:38
- Kuti musalowe m'kuyesedwa: Luka 22:40-46
- Omwe akukunyozani (adani anu): Luka 6:28
- Oyera mtima onse: Aefeso 6:18
- Odwala: Yakobo 5:14
- Wina ndi mnzake (kunyamulirana zothodwetsa wina ndi mnzake): Yakobo 5:16
- Amuna onse, mafumu, ndi iwo amu ulamuliro: 1 Timoteyu 2:1-4
- Zosowa za tsiku ndi tsiku: Mateyu 6:11
- Nzeru: Yakobo 1:5
- Machiritso: Yakobo 5:14-15

- Chikhululukiro: Mateyu 6:12
- Chifuniro cha Mulungu ndi Ufumu wake ukhazikitsidwe: Mateyu 6:10
- Kupumulitsidwa ku mazunzo: Yakobo 5:13

PEMPHERANI MALONJEZANO

Mupempha, ndipo simulandira, popeza mupempha koipa, kuti mukacimwaze pocita zikhumbitso zanu. (Yakobo 4:3)

Mulungu amayankha mapemphero molingana ndi malonjezano ake. Mukamapempha mosemphana ndi malonjezanowa, pemphero lanu siliyankhidwa. Zili monga momwe tate akhalira ndi ana ake. Munthu sampatsa mwana wake wang'ono chirichonse apempha. Amaonetsetsa kuti zina zichitike koma zina ayi. Mu njira imeneyi tateyo amapereka zinthu zina mwana akapempha ndipo zina samupatsa.

Izi zili chimodzimidzi ndi Mulungu. Wapereka malonjezano kwa ife ndipo malonjezanowo amatitsogolera momwe tingaperekere zopempha zathu kwa Iye. Mukuyenera kudziwa malonjezano a Mulungu. Mukatero, pempherani molingana ndi malonjezanowo. Njira imodzi yomwe mungatsate pochita izi ndiko kudula mzere malo ena alionse pomwe pali vesi ya malonjezano. Gwiritsani ntchito Baibulo lanu popemphera molingana ndi mavesi a malonjezano aja.

ZOTCHINGA ZA PEMPHERO

- Tchimo la mtundu uliwonse: Yesaya 59:1-2; Masalimo 66:18; Yesaya 1:15; Miyambo 28:9
- Mafano a mu mtima: Ezekiele 14:1-3.
- Mzimu wosakhulukira: Marko 11:25; Mateyu 5:23
- Kudzikonda, zokhumba zolakwika: Miyambo 21:13; Yakobo 4:3.
- Njala yofuna maudindo, mapemphero olakwika: Yakobo 4:2-3.
- Kusakhala bwino ndi wokondedwa wanu: 1 Petro 3:7
- Kudzimva kukhala wolungama: Luka 18:10-14.
- Kusakhulupirira: Yakobo 1:6-7.

- Kusakhala mwa Khristu ndi Mau ake: Yohane 15:7
- Kusowa chifundo: Miyambo 21:13.
- Chinyengo, kunyada, kupemphera mobwereza-bwereza: Mateyu 6:5; Yobu 35:12-13.
- Kusapemphera molingana ndi chifuniro cha Mulungu: Yakobo 4:2-3.
- Kusapempha mu dzina la Yesu: Yohane 16:24
- Zotchinga za ziwanda za Satana: Daniele 10:10-13; Aefeso 6:12.
- Kusafuna kaye Ufumu wa Mulungu: Ndi pokha-pokha mwafuna kaye Ufumu wa Mulungu kuti “zina zonse” zidzakutsatani: Mateyu 6:33.
- Mulungu atha kukhala ndi cholinga chachikulu pa inu pamene akukukanizani zomwe mwapemphazo: 2 Akorinto 12:8-9.
- Mukapanda kudziwa momwe mungapempherere, pemphero limatchingidwa. Apa ndi pomwe pamafunika kumlola Mzimu Woyera kuti apemphere kudzera mwa inu: Aroma 8:26.

NTHAWI YOSAFUNIKA KUPEMPHERA

Ndi bwino kuphunzira kudikira pa Ambuye m’pemphero kuti akutsogolereni musanachite kalikonse. Komanso ndi zofunika kudziwa nthawi yoti simukufunika kupemphera koma kuchita. Mulungu akupatsani mwayi woti muchite kanthu, chitani, osati kupitiriza kupemphera.

Mwa chitsanzo, pa madzi owawa aku ku Mara pamene Mose analilira kwa Ambuye, Mulungu anamuuza Mose chochita kuti madzi akhale okoma. Panalibenso chifukwa chomadikira pa Ambuye m’pemphero. Mose anayenera kuchita mwamsanga zomwe Mulungu wabvumbulutsa. Chimodzimodzinso Yoswa, pamene anapemphera za kugonjetsedwa koopsa kwa Israel ndi Ayi. Mulungu anabvumbulutsa kuti pali tchimo pakati pa ana a Israel. Anamuuza Yoswa kuti...

Dzuka, ugoneranjani pa nkhope pako? Israel wachimwa.... Dzuka, yeretsa Israel (Yoswa 7).

Sinali nthawi yopemphera. Inali nthawi yoti achite malangizo omwe wauzidwa m’pemphero ndi Mulungu. Anthu ena amagwiritsa ntchito pemphero ngati pothawira kuti asachitepo kanthu pa zomwe Mulungu wawauza kuti achite.

Enanso amapitirirabe kupemphera koma Mulungu atayankha kale posasangalala ndi yankholo. Onani nkhani ya Balaam mu Numeri 22 makamaka mavesi a 18-22. Balaam analibe chifukwa

chokwanira kupita kwa Mulungu ndi yomweyo popeza Mulungu anali atamletsa kale kuti asatengepo pa zomwe zikuchitikazo (onani vesi 12).

KUSALA KUDYA

Kusala kudyā ndi gawo lachinayi la nkondo. Kumachitika pamodzi ndi pemphero pamene mu kumenya nkondo mu dziko lauzimu.

TANTHAUZO LA KUSALA KUDYA:

Kusala kudyā ndi kukhala osadya.

MITUNDU YA KUSALA KUDYA:

Molingana ndi Mau a Mulungu, pali mitundu iwiri ya kusala kudyā. Kusala kwa tunthu ndi kusala moyepula. Kusala kwatunthu ndi pomwe munthu sakudyā kapena kumwa chiri chonse (Machitidwe 9:9). Kusala moyepula ndi pomwe munthu amangodyako tina ndi tina basi (Daniel 10:3).

KUSALA KUDYA KOWONEKERA NDI KWA MSERI

Kusala kudyā ndi nkhani ya pakati pa munthu ndi Mulungu. Imachitika mseri osati kumalengeza:

Ndipo Simoni Petro anayankha nati, Inu ndinu Kristu, Mwana wa Mulungu wamoyo. Ndipo Yesu anayankha iye, nati, Ndiwe wodala, Simoni Bar-Yona: pakuti thupi ndi mwazi sizinakuululira ici, koma Atate wanga wa Kumwamba. Ndiponso Ine ndinena kwa iwe, kuti iwe ndiwe Petro, ndipo pa thanthwe ili ndidzakhazika Mpingo wanga; ndipo makomo a dziko la akufa sadzaulaka uwo. (Mateyu 6:16:18).

Atsogoleri atha kulengeza dongosolo losala kudyā la mpingo wonse:

Ombani lipenga m'Ziyoni, patulani tsiku losala, lalikirani msonkhano woletsa, (Yoweli 2:15).

CHOLINGA CHA KUSALA KUDYA

Pali zolinga zeni zeni zauzimu zosalira kudyā. Nkofunika kumvetsa bwino zimenezi, popeza ngati musala kudyā ndi zolinga zolakwika simupindula kanthu.

Werengani mavesi ali m'musiwa pa zolinga zosalira kudyā. Mavesiwa amabvumbulutsa mphamvu yodabwitsa ya kusala kudyā mu nkondo yauzimu. Munthu amasala kudyā kuti:

- Adzichepetse yekha: Masalimo 35:13; 69:10
- Alape machimo: Yoweli 2:12
- Kuti mulandire bvumbulutso: Daniel 9:2; 3:21-22
- Kumasula magoli a uchimo, kuchotsa zolemetsa, kumasula msinga, kuphwanya magoli: Yesaya 58:6
- Kudzetsa osauka kuthupi ndi kuuzimu komwe: Yesaya 58:7
- Kuti pemphero limveke kwa Mulungu: 2 Samueli 12:16,22; Yona 3:5,10.

Kusala kudya sikumasintha Mulungu. Imasintha inu. Mulungu amachita nanu molinga ndi ubale womwe muli nawo ndi Iye. Mukasintha, machitidwe a momwe Mulungu amachitira ndi inu adzasinthanso. Simusala kudya kuti musinthe Mulungu, chifukwa Mulungu sasintha. Werengani bukhu la Yona kuti muone momwe izi zinachitikira ku Nineve.

KUTALIKA KWA NTHAWI YOSALA KUDYA

Kutalika kwa nthawi yosala kudya kumatengera momwe Mulungu walankhulira mu mtima mwanu. Mulungu angathe kukutsogolerani kuti musale nthawi yochepa kapena yaitali. Kumbukirani nkhani ya Esau ndi Yakobo. Yakobo amaphika chakudya choti adye koma ataona kuti pali mwayi wotenga ukulu, analolera kupereka chakudya ndi kukhala ndi njala. Kodi Esau akanasala chakudya chimenechi sizikanakhala bwino kodi?

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Ndi ndondomeko ziti zimene zimamasula mphamvu ya Mulungu miyoyo ya okhulupirira?

_____ndi_____

3. Ndi milingo iti itatu ya pemphero yomwe yafotokozedwa muphunzirori?

4. Lembani mitundu itatu yapemphero imene yafotokozeredwa

5. Lembani zontchinga zina za pemphero zomwe zakambidwa mu chaputalachi.

6. Perekani tanthauzo la pemphero.

7. Perekani tanthauzo la kusala kudya.

8. Ndi mitundu iti iwiri yakusala kudya?

_____ndi_____

9. Lembani mwachidule zolinga zakusala kudya.

(Mayankho amayesowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Mayankho a mapemphero amaperekedwa:

- Pena nthawi yomweyo: Yesaya 65:24; Danieli 9:21-23
- Pena mochedwa: Luka 18:7
- Pena mosemphana ndi zokhumba zathu: 2 Akorinto 12:8-9
- Mopilira chiyembekezo chathu: Yeremiya 33:3; Aefeso 3:20

Kumbukirana. Pemphero la Yesu munda wa Getsemani silinasithe cholinga cha Mulungu, koma chifuniro cha Mulungu chinakhala poyera(Ahebri 5:7-9). Mapemphero athu sikuti samayakhidwa. Chifukwa chakuti amayakhidwa munjira imene ife sitimayembekezera. Chomwe timawona ngati mapemphero osayakhidwa nthawi zambiri amakhala ndi cholinga chachikulu.

2. Pamene tikupemphera molingana ndi ndondomeko za pemphero la Ambuye limalimbikitsa kukhala ndi chithuzithuzi chabwino.

Pamene tikupemphera...	Timawonetsera
Atate wanthu Wakumwamba...	Chikhalidwe chaumwana
Dzina Lanu Liyetsedwe...	Malingaliro opereka ulemu
Ufumu wanu udze	Malingaliro oyembekezera
Kufuna kwanu kuchitidwe pano	
Padziko lapansi ndikumwamba	Malingaliro ongonjera
Mutipatse ife lero chakudya chanthu	
Cha lero	Malingaliro odalira
Mutikhululukire zochimwa zanthu	Malingaliro olapa
Monga tiwakhululukira adani anthu	Malingaliro okhululukira
Musatitengere ife kokatiyesa koma	
Mutipulumutse ife kwa oipawo	Malingaliro achipambano
Wanu ndi ufumu, mphamvu,ndi ulemerero	

3. Werengani Yakobo 5:17-8. Imeneyi ndi ndodnomeko ya pemphero la mphamvu ndi chikhulupiriro chifukwa:
- Limakhazikika pa malonjezano a Mulungu : 1Mafumu 18:1
 - Limakwaniritsa mulingo wa lonjezano :1 Mafumu 18:2
 - Amateteza posatengera uthenga umene wabwera :1 Mafumu 18:43
4. Werengani zitsanzo zotsatiriza za mapemphero amphamvu amene analembedwa mu Baibulo:

Genesisi

Chiyambi cha mbiri ya pemphero: 4:26

Kupitirira kwa pemphero ndi uzimu : 5:21-24

Pemphero ndi Guwa :12-13

Pemphero la wolowa mmalo :15

Pemphero, chiyakhulo chakulira :16

Pemphero la kumzinda woipa : 18-19

Pemphero kutsatira kusawonetsetsa :20

Pemphero lakumvera: 22

Pemphero la mkwati : 24

Pemphero lazimayi osabereka : 25:19-23

Pemphero lositha zinthu : 26

Pemphero monga malumbiro : 20

Pemphero la kwa bale wolakwiridwa : 32

Pemphero, moto wobisika: 39-41; 45:5-8; 50:20,24

Pemphero lodalitsa mafuko : 48-49

Eksodo

Pemphero lawonetseredwa ngati kulira: 1-2

Pemphero ngati kukambirana: 3-4

Pemphero ngati kudandaula: 5-7

Pemphero ngati kutamanda: 1-5

Pemphero pa mabvuto: 17

Pemphero la osowa: 22:22-24

Pemphero pakuchedwetsedwa kwa chigamulo chofunika: 32

Pemphero loyamba la Mose kwa Aisraeli: 32:9-14

Pemphero lachiwiri la Mose: 32:30-34

Pemphero lachitatu la Mose: 33:12-23

Pemphero ndikusandulidwa: 34

NUMERI:

Pemphero ngati mdalitso: 6:24-27

Pemphero lakusunga ndi kuteteza: 10:35-36

Pemphero lochotsa chiweruzo: 11:1-2

Pemphero la munthu ofatsa: 12

Pemphero lopempha kulowerera kwa kumwamba kulimbana ndi kuukira: 16

Pemphero lopulumutsa ku imfa: 21

Pemphero ndi uneneri: 23-24

Pemphero kwa mtsogoleri wa tsopano: 27

DEUTERONOMO:

Pemphero pa zochitika zapaderadera: 3:23-29

Pemphero la amene alipamwamba: 4:7

Pemphero loti chiweruzo chikhalebe: 9:20, 26-29

Pemphero monga mdalitso: 21:6-9

Pemphero monga kuyamika: 26

Pemphero ngati nyimbo: 32-33

YOSWA:

Pemphero ngati chobetchera: 5:13-15

Pemphero lomwe Mulungu samayakha: 7

Pemphero lolekereredwa ndi zotsatira zopanda pake: 9:14

Pemphero limene limabereka chozizwa: 10

OWERUZA:

Pemphero lachitsogozo: 1

Pemphero mu nthawi ya nkhondo: 4-5

Pemphero lazizindikiro: 6

Pemphero mu nthawi ya mavuto: 10-10-16

Pemphero ngati kuchonderera: 11:30=40

Pemphero la mwana wosabadwa: 13

Pemphero pokumana ndi imfa: 16:23-28

Pemphero loyakhidwa mwachindunji: 20:23-28

Pemphero la kwa mtundo otaika: 21:2-3

1 SAMUELI

Pemphero lopanda mau: 1

Pemphero, kunenera kuchitika poyera: 2:1-10

Pemphero mmalo oyera: 3

Pemphero ku mavuto adziko: 7

Pemphero kwa mfumu: 8

Pemphero lobisidwa: 12

Pemphero la mfumu yosautsika: 14

Pemphero la mtima wolira: 15:11

Pemphero ngati mau aang'ono: 16:1-12

Pemphero ngati chisisi chobisika: 17

Pemphero ngati kufunsira: 23

Pemphero kwa makuto ogotha: 28:7

Pemphero lobwezeretsa zimene zinaonongeka ndi nkondo: 30

2 SAMUELI:

Pemphero la chizindikiro chachigonjetso: 5:19-29

Pemphero la madalitso pa nyumba ndi ufumu: 7:18-29

Pemphero kwa mwana wodwala: 12

Pemphero ngati kungonyengezera: 5:7-9

Pemphero ngati Salimo: 22

Pemphero lomvomereza kuzikuza: 24:10-17

1 MAFUMU:

Pemphero la mtima wa nzeru: 3

Pemphero lopatula: 8:12-16

Pemphero lamkono wolumala: 13:6

Pemphero la miyamba yotsekeka: 17

Pemphero la chiukitso cha mwana womwalira: 17:20-24

Pemphero lopereka ulemu kumwamba: 18:16-41

Pemphero ndi chipiriro: 18:45

Pemphero la kwa akumfa: 19

2 MAFUMU:

Pemphero la mwana wakufa: 4:32-37

Pemphero la masopenya: 6:13-17

Pemphero lachipulumutso kwa anthu opusa: 19

Pemphero la moyo wautali: 20:1-11

1 MBIRI:

Pemphero lakulemera ku uzimu: 4:9-10

Pemphero chifukwa cha mantha: 13:12

Pemphero loyakhidwa ndi moto: 21

Pemphero ngati chiyamiko: 23:30

Pemphero ndikupereka: 29:10-19

2 MBIRI:

Pemphero la choopsya cha dziko: 14:11

Pemphero ndi kusitha: 15

Pemphero ndi kupemphanso mbiri: 20:3-13

Pemphero lobwezeretsa: 33:13

EZARA:

Pemphero lachiyamiko: 7:27-28

Kupemphera ndi kusala kudya: 8:21-23

Pemphero ndi kumvomereza: 9:5-10:4

NEHEMIYA:

Pemphero lobadwa chifukwa chamavuto: 1:4-11

Pemphero pampanipani: 2:4

Pemphero lachipulumutso kuchitozo: 4:1-6

Pemphero logonjetsera mkwiyo: 4:7-9

Pemphero lolimbana ndi zaufiti: 6:9-14

Pemphero ndi Mau: 8:1-13

Pemphero ndi ubwino wa Mulungu: 9

Pemphero lachikumbukiro: 13:14, 22, 29, 31

YOBU:

Pemphero losiya: 1:20-22

Pemphero lomvetsa chisoni: 6:8-9; 7:17-21

Pemphero lolungamitsidwa: 9

Pemphero lolimbana ndi kusakhulupirika: 9

Pemphero ndi phindu: 21:14-34

Pemphero ndi chifukwa: 23

Pemphero loyakhidwa ndi kamvulumvulu: 38

Pemphero monga akupembedzera: 42:7-10

MASALIMO:

Pemphero lobadwa mukuukira: 3

Pemphero lachiyero: 4

Pemphero lopempha machitachita akumwamba: 7

Pemphero lotamanda chifukwa chakulowerera kwakumwamba: 8

Pemphero la mtanda: 22

Pemphero la chisamaliro cha m'busa: 23

Pemphero lakuwonetsera kwa ulemerele wakumwamba: 24

Pemphero loti kumwamba kumvomereze: 25

Pemphero la mtima okhulupirira: 27

Pemphero ngati chodalira cha Kristu 31

Pemphero la moyo wasokonezeka: 32

Pemphero la chitetezo kwa adani: 35

Pemphero lotamanda pa chikondi chosatha: 36

Pemphero la anthu oyenda: 39, 90, 91

Pemphero mmavuto akulu: 41

Pemphero monga khomo la chiyembekezo: 42-43

Pemphero la chithandizo lakumwamba: 44

Pemphero lobisalako: 46

Pemphero la mtima wasweka: 51

Pemphero mu nthawi zonse: 55

Pemphero lodalira: 71

Pemphero kwa Mulungu Mwini: 73

Pemphero la matando ku ukulu wa Mulungu: 96

Pemphero lothawa mayesolo: 102-103, 105

Pemphero lachikumbutso: 106

Pemphero la onse amene akukumana ndi zovuta pa Nyanja: 107

Pemphero ndikutsimikizira kwa Malemba: 19, 119

Pemphero ku mtima ofunafuna: 139

MIYAMBO:

Bukuli limakhazikika pa pemphero monga ngati njira imene Mulungu amaperekera nzeru.

MLALIKI:

Bukuli limafotokoza pemphero mokhudzana ndi kuwopsa.

NYIMBO YA SOLOMONI:

Zinsisi za pemphero: Buku lonse.

YESAYA:

Pemphero lomwe Mulungu samamva: 1:15; 16:12

Pemphero ndi kuyeretsedwa: 6

Kupempherera chizindikiro: 7:11

Pemphero lokweza: 12

Pemphero lotamanda chifukwa chachipambano: 25

Pemphero la mtendere: 26

Pemphero ndi kutsimikizika: 41

Pemphero ndi zochitika: 55

Pemphero silimadziwika kwa ambiri: 59

Pemphero lowonetsera mphamvu ya kumwamba: 63-64

YEREMIYA:

Pemphero lovomereza kusakwanitsa: 1

Pemphero monga kulira chifukwa chobwerera mbuyo: 2-3

Pemphero lodandaula: 4: 10-31

Pemphero lolira chifukwa choukira: 5

Pemphero lochokera kundende: 6

Pemphero lokanidwa: 7:16

Pemphero lachilungamo: 10:23-25

Pemphero lopulumutsa ku tchimo ndi chilala: 14:7-22

Pemphero loti kumwamba kubwezere: 15:15-21

Pemphero la chisokonezo kwa adani: 16: 19-21; 17:13-18

Pemphero logwetsa uphingu olakwika: 18:18-23

Pemphero la mtima wothodwa: 20:7-13

Pemphero lothokoza chifukwa chakukoma mtima kwakumwamba: 32:16-25

Pemphero la okhulupira otsala: 42

MALIRO:

Pemphero la ululu: 1:20-22

Pemphero lodandaula: 2:19-22

Pemphero ngati kudandaula: 3

Pemphero la oponderezedwa: 5

EZEKIELI:

Pemphero ngati chiwonetsero: 4:14

Pemphero la chitetezo ku zotsarira: 9:8-11

Pemphero la mmalo oyera: 11:13-16

DANIELI:

Pemphero lomasulira: 2:17-18

Pemphero lonyozera lamulu: 6:10-15

Pemphero lovomereza: 9

Pemphero ndi zotsatira zake za uzimu: 10

Pemphero lokhudzana ndi machenjerero amoyo: 12:8-13

HOSEYA:

Mulungu kudandaulira dziko lobwerera mbuyo kuti lipemphere pemphero lakulapa.

YOWELI:

Pemphero muzobwera mwadzidzidzi: 1:19-20

Pemphero ndi kulira: 2:17

AMOSI:

Pemphero lakulapa ndi chikhululukiro.

YONA:

Pemphero la anthu amene amayenda panyanja: 1:14-16

Pemphero lotulutsa anthu ku Jahena: 2

Pemphero lolapa kwa mzinda: 3

Pemphero la neneri okhumudwa: 4

MIKA:

Pemphero ndikudikira pa Ambuye kuti akwaniritse Mau Ake.

HABAKUKU:

Pemphero lodandaula ndi kubisibwa: 1:1-4, 12-17

Pemphero lachikhulupiriro: 3

MALAKI:

Pemphero –kuchita chiwonetsero 1: 1:2

Pemphero- kuchita chiwonetsero 2: 1:6

Pemphero – kuchita chiwonetsero 3: 1:7, 13

Pemphero – kuchita chiwonetsero 4: 2:17

Pemphero – kuchita chiwonetsero 5: 3:17

Pemphero – kuchita chiwonetsero 6: 3:8

MATEYU:

Pemphero ndi kufunika kokhululukira: 5:22-26; 6:12, 14-15

Pemphero ndi chinyengo: 6:5-7

Pemphero monga mmene anaphunzitsira Yesu: 6:8-13

Pemphero momwe linatsimikizilidwira ndi Yesu: 7:7-11

Pemphero la wakhate: 8:1-4

Pemphero la Kenturiyo: 8:5-13

Pemphero munamondwe: 8:23-27

Pemphero la ogwida ndi ziwanda: 8:28-34

Pemphero la Yayiro: 9:18-19

Pemphero la mzimayi wodwalika: 9:20-22

Pemphero la amuna akhungu: 9:27-31

Pemphero la antchito: 9:37-39

Pemphero lothokoza la Yesu Kristu kwa Mulungu: 11:25-27

Pemphero la pa phiri: 14:23

Pemphero la Petro masautso: 14:28-30

Pemphero la mkazi wa kukanani: 15:21-28

Pemphero kwa mwana wodwala khunyu: 17:14-21

Pemphero mu gwirizano: 18:19-20

Pemphero mu faniziro: 18:23-25

Pemphero lofuna malo abwino: 20:20-28

Pemphero lochiza akhungu: 20:29-34

Pemphero la chikhulupiriro: 21:18-22

Pemphero loziyenereza: 23:14, 25

Pemphero la matalente: 25:20, 22, 24

Pemphero lomaganizo ozipereka: 26:26, 36-46

Pemphero la Pakavari: 27:46, 50

MARKO:

Pemphero lotulitsira ziwanda: 1:23-28, 32-34

Pemphero ndi chikhalidwe cha Kristu: 1:35; 6:41, 46

Pemphero kwa osamva ndi wosalakhula: 7:31-37

Pemphero ndi kusala kudya: 2:18; 9:29

Pemphero la mnyamata mwini chuma chambiri: 10:17-22

LUKA:

Pemphero la Zakaliya: 1:8, 13, 67-80

Pemphero lolambira: 1:46-55

Pemphero lotmanda: 2:10-20, 25-38

Pemphero pakuyambika kwa ntchito: 3:21-22

Pemphero pakuthawa kukutchuka: 5:16

Pemphero la nkhumu ndi modzi: 6:12-13, 20, 28

Pemphero ndikusandulitsidwa: 9:28-29

Pemphero mu chifaniziro: 11:5-13

Pemphero kwa olowerera: 15:11-24, 29-30

Pemphero lotulukira Ku Jahena: 16:22-31

Pemphero la akhate khumi: 17:12-19

Pemphero lobwera mwafanizo: 18:1-8

Pemphero la Mfalisi ndi wamsokho: 18:9-14

Pemphero lachitetezo cha Petro: 22:31-31

Pemphero lazowawa: 22:39-46

Pemphero ndi kuuka kwa Ambuye: 24:30, 50-53

YOHANE:

Pemphero la uzimu: 4:9, 15, 19, 28; 7:37-39; 14:16

Pemphero la munthu wolungama: 4:46-54

Pemphero la mkate wa moyo: 6:34

Pemphero lotsimikiza: 11:40-42

Pemphero lokhala ndizolinga ziwiri: 12:27-28

Pemphero monga mwayi: 14:13-15; 15:16; 16:23-26

Pemphero la mapemphero onse: 17

MACHITIDWE:

Pemphero pa chipinda chapamwamba: 1:13-14

Pemphero la mulowa mmalo: 1:15-26

Pemphero ndi kulambira: 2:42-47

Pemphero ngati kuyang'anira: 3:1

Pemphero lakulimba mtima kuchitira umboni: 4:23-31

Pemphero ndi utumiki waku dziko: 6:4-7

Pemphero la ophedwa woyamba: 7:55-60

Pemphero kwa Samariya ndi anyanga: 8:9-25

Pemphero la otembenuka: 9:5-6, 11

Pemphero kwa Dokasi: 9:36-43

Pemphero la Koneriyo: 10:2-4, 9, 31

Pemphero kwa Petro m'ndende: 12:5, 12-17

Pemphero lopatulira: 13:2-3, 43

Pemphero ndi kusala kudya: 13:2-3; 14:15, 23, 26

Pemphero muphepete mwatsinje: 16:13,16

Pemphero mundende: 16:13, 16

Pemphero lozipereka: 20:36

Pemphero pakuphwasuka kwa ngalawa: 27:33, 35

Pemphero kwa wodwala malungo ndi kamwazi: 28:8, 15, 28

AROMA:

Pemphero la ulendo opambana: 1:8-15

Pemphero lolimbikitsidwa ndi Mzimu: 8:15, 23, 26-27

Pemphero chifukwa cha Israeli: 10:1, 11:26

Pemphero monga ngati kupitiriza utumiki: 12:12

Pemphero la anthu ofanana maganizo: 15:5-6, 30-33

Pemphero logonjetsera satana: 16:20, 24-27

2 AKORINTO:

Pemphero la mdalitso: 1:2-4

Pemphero loti amuchotsere munga: 12:7-10

AEFESO:

Pemphero ndi malo a okhulupirira: 1:1-11

Pemphero lopempha mphamvu: 1:15-20

Pemphero monga ngati njira yomufikira Mulungu: 2:18; 3:12

Pemphero lofuna kukhala okhutitsidwa: 3:13-21

Pemphero lotetezera ankhondo: 6:18-19

AFILUPI:

Pemphero lopempha chisangalalo: 1:2-7

Pemphero ndi mtendere wammaganizo: 4:6-7, 19-23

AKOLOSE:

Pemphero lotambanda chifukwa chaulemero: 1:1-8

Pemphero la magulu amadalitso asanu ndi awiri: 1:9-14

Pemphero la chiyanjano: 4:2-4, 12, 17

1 ATESALONIKA:

Pemphero lachikumbutso: 1:1-3

Pemphero la ulendo obwerera: 3:9-13

Pemphero, matamando, ndi kulungamitsidwa: 5:17-18, 23-24, 28

2 ASETALONIKA:

Pemphero lamaitanidwe: 1:3, 11-12

Pemphero la chithonhozo ndi kukhazikika: 2:13, 16-17

Pemphero la Mau ndi chitetezo: 3:1-5

2 TIMOTEO:

Pemphero lopempherera utumiki wa Timoteo: 1:2-7

Pemphero lopempherera nyumba ya Onesiforo: 1:6-18

Pemphero kwa abwenzi onama: 4:14-18

AHEBRI:

Pemphero la matamando chifukwa chachilengedwe: 1:10-12

Pemphero lopempha chifundo ndi kukonderedwa: 4:16

Pemphero ndi utumiki wa Yesu: 5:7-8; 7:24-25

Pemphero lofuna kugwira ntchito muchifuniro cha Mulungu: 12:9, 12, 15

Pemphero lofuna kukhala wolungama: 13:20-21

YAKOBO:

Pemphero lopempha nzeru: 1:5-8, 17

Pemphero lophonya cholinga: 4:2-3

Pemphero limene limapambana: 5:13-18

1 PETRO:

Pemphero lothokoza chifukwa chacholowa: 1:3-4

Pemphero la makhalidwe a m'banja: 3:7-12

Pemphero-kuyang'anira: 4:7

Pemphero lokhazkika kwa Akhristu: 5:10-11

2 PETRO:

Pemphero loti chisomo ndi mtendere zichiluke: 12

3 PETRO:

Pemphero kukhala msana wa mbiri yabwino: 1-4, 12

YUDA:

Pemphero muuzimu: 20

CHIBVUMBULUTSO:

Pemphero lotamanda Mwana wa Khonsa chifukwa cha chiwombolo: 5:9

Pemphero monga ngati chofukiza chagolide: 5:8; 8:3

Pemphero la onse ophedwa: 6:10

Pemphero la amitundu: 7:9-12

Pemphero la akuluakulu: 11:15-19

Pemphero la Mose: 15:3-4

Pemphero la oyera mtima okwezedwa: 19:1-10

Pemphero lotsekera Baibulo: 22:17, 20

CHAPUTALA 14

NDONDOMEKO YA MPHAMVU 8:

MPHAMVU YA MAU

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsolera osawonera.
- Kufotokoza kumene kumachokera mau a mphamvu.
- Kupereka tanthauzo la mau awa “rhema” ndi “logos” mau a Mulungu.
- Kufotokoza mmene Yesu anakumanirana ndi mayesero a satana kupyolera mu mau a mphamvu.
- Kufotokoza udindo wanu ku mau a Mulungu.
- Kulemba mwachidule zolinga za mphamvu za mau a Mulungu.
- Kufotokoza chifukwa chani mau anu ndiofunika kumphamvu ya uzimu.

VESI YOTSOGOLERA:

Pakuti Mau a Mulungu ali amoyo ndi ochitachita, ndi akuthwa koposa lupanga lakuthwa konse konse, napyoza kufikira kugawira moyo ndi mzimu, ndi mfundo ndi mafuta a m'mafupa nazindikiritsa zolingalira ndi zitsimikizo za mtima.(Ahebri 4:12)

MAU OYAMBA

Baibulo ndi mau olembedwa a Mulungu. Muli mphamvu yapaderadera mau a Mulungu.

Pakuti mau a Mulungu ali amoyo, ndi ocitacita, ndi akuthwa koposa lupanga lakuthwa konse konse, napyoza kufikira kugawira moyo ndi mzimu, ndi zimfundo ndi mafuta a m'mafupa, nazindikiritsa zolingirira ndi zitsimikizo za mtima. (Ahebri 4:12)

momwemo adzakhala mau anga amene aturuka m'kamwa mwanga, sadzabwerera kwa Ine cabe, koma adzacita cimene ndifuna, ndipo adzakula m'mene ndinawatumizira. (Yesaya 55:11)

Simungalandire chidzalo cha mphamvu ya Mulungu pokhapokha mutakuma kaye ndi mphamvu ya Mau Ake.

KUCHOKERA MAU

Mulungu ndiye kochokera mphamvu ndi Mau Ake olembedwa. Izi zimapangitsa mau a Mulungu kukhala a mphamvu.

Ambuye anapatsa mau: Akazi akulalikira uthengawo ndiwo khamu lalikuru. (Salima 68:11)

Ndipo mwa icinso ife tiyamika Mulungu kosalekeza, kuti, pakulandira mau a Uthenga wa Mulungu, simunawalandira monga mau a anthu, komatu monga momwe ali ndithu, mau a Mulungu, amenenso acita mwa inuokhulupirira. (1 Atesalonika 2:13)

Mulungu analenga dziko ndi Mau Ake:

Zakumwamba zinalengedwa ndi mau a Yehova; Ndipo ndi mpweya wa m'kamwa mwace khamu lao lonse. (Masalimo 33:6)

Mulungu akupitirizabe kugwira dziko lonse ndi zinthu zonse mmene ziriri ndi mphamvu ya Mau Ake:

ameneyo, pokhala ali cinyezimiro ca ulemerero wace, ndi cizindikilo ceni ceni ca cikhaliidwe cace, nanyamula zonse ndi mau a mphamvu yace, m'mene adacita ciyeretso ca zoipa, anakhala pa dzanja lamanja la Ukulu m'Mwamba, (Ahebri 1:3)

“RHEMA” NDI “LOGOS”

Pali mau awiri osiyana a Chigriki amene agwiritsidwa ntchito m’Baibulo pa mau a Mulungu. Amodzi mwa mawuwa ndi “logos” ndipo amatanthauza kuti kuyakhula kwamphuphu kwa Mulungu. Liwu lachiwiri ndi “Rhema,” lomwe limatanthauza kuti zoyankhula za Mulungu zapaderadera zomwe zimagwiritsidwa ntchito pa zochika zapaderadera. ‘Logos’ bvumbulutso la mau a Mulungu ndi la mphamvu, koma pamene Mulungu wadzutsa “rhema” mumau Ake olembedwa, amenewa amakhala amphamvu mwapaderadera.

Pamene Mulungu wadzutsa “rhema”, vesi imene mwawerenga nthawi zambiri mbuyomu imayamba kukupatsani tanthauzo latsopano. Mutha kuwona kuti imagwiritsidwa ntchito

mwapaderadera pa zomwe mukukumana nazo. Mau a “rhema” amakupatsani yankho, bvumbulutso, kapenaso chithonhozo chimene mukufuna panthawi imeneyo.

KUYESEDWA KWA YESU

Mphamvu ya Mulungu inaperekedwa kwa Yesu Kristu koma mphamvu imeneyi inayera kuyesedwa chifukwa mphamvu zimachulukuka ukakhala pampanipani. Kulimbana kwakukulu kwapakati pa mphamvu ya Yesu ndi mphamvu ya satana kunachitika kumayambiriro kwa utumiki wa Kristu. Tisanapitirire ndi mphunzirori, werengani kaye zazimezi mu Mateyu 4:1-11; Marko 1:12-13; ndi Luka 4:1-13.

Poyamba, satana anayesera kumuyesa Yesu kuti asandutse mala kukhala mkate. Mphamvu ya Yesu imene posachedwa inasandutsa madzi kukhala vinyo inakathaso kusandutsa mala kukhala mkate. Koma kuchita zimenezi panthawi imeneyi anakakhala kuti akuchita zimenezi mwayekha popanda Mulungu ndipo kunakakhala kugwiritsa ntchito mphamvu Zake kuti apindule Iye mwini.

Kachiwiri, satana anayesa kumuyesa Yesu kuti aziponye Yekha pansu kuchokera pamwamba pa kachisi kuti awonetsera mphamvu Zake. Satana anagwiritsa ntchito udyo malemba ndi cholinga chomupusitsa Yesu, zinali zabwino kutero.

kachita satana anamuyesa Yesu pomulonjeza mphamvu za dziko lapansi. Satana anamuza kuti azampatsa m ufumu onse a dziko lapansi ngati Yesu angamulambire iye.

Muzonse zochitikazi pofuna mphamvu, Yesu anakumana ndiyesero ndi mau a Mulungu. Yesu anatenga mau amene anali ogwirizana ndi nthawi imene anali. Anagwiritsa ntchito “rhema” mau a Mulungu.

KUGWIRITSA NTCHITO MAU AMPHAMVU

Sikokwanira kungozindikira kuti muli mphamvu mu mau a Mulungu. Kuti akhale aphindu, mau amanewo akuyenera kugwiritsidwa ntchito monga mmene Yesu anachitira. Yesu anawonetsera mwachindunji kuti mau amene ayakhula sanali Ake. Anali Mau a Mulungu (Yohane 3:32; 14, 24; 17:8, 14)

Yesu anayakhula Mau a Mulungu ndi mphamvu:

cifukwa mau ace anali ndi ulamuliro. (Luka 4:32)

Ndipo anthu onse anadabwa, nalankhulana wina ndi mnzace, nanena, Mau amenewa ali otani? cifukwa ndi ulamuliro ndi mphamvu angolamulira mizimu yonyansa, ndipo ingoturuka. (Luka 4:36)

Yesu anayakhula Mau a Mulungu kwa munthu amene anali ndi dzanja lopuwala ndipo linachiritsidwa (Marko 3:1-5). Anayakhula Mau kwa wakhate ndipo anachiritsidwa (Mateyu 8:2-3). Anati...

- “tauka” kwa munthu wopuwala pa thamando (Yohane 5:8)
- “kuwona” kwa akhugu (Luka 7:21)
- “tuluka” kwa ziwanda (Mateyu 9:32-33)
- “kumva” kwa osamva (Marko 7:32-35)
- “chiukitso” kwa akufa (Marko 11:44)

Yesu anazindikira kuti muli mphamvu mu mau a Mulungu, komaso anazindikira kuti munthu akuyenera kumva ndi kuchitapo kathu ku Mawuwo ndi cholinga choti akhale ophindu. Mau a Yesu, amene analinso Mau a Mulungu, anali amphamvu mokuti amatha kugwira ntchito ali kutali. Yesu sankayenera kupezeka pamalo pamene pali bvuto. Munthu wina amene anali ndi wantchito amene amkadwala anati...

Ndipo Yesu anatambalitsa dzanja lace, namkhudza iye, nati, Ndifuna; takonzedwa. Ndipo pomwepo khate lace linacoka. (Mateyu 8:8, 13)

Munthu ameneyu anakhulupirira Mau amphamvu a Mulungu. Anadziwa kuti mphamvu zake sizingasokonezedwe chifukwa cha nthawi, malo, kapena chotchinga chilichonse cha munthu. Kuma kuti akhale ophindu mmoyo ndi nyengo zake, amayenera kuwafusa. Akuyenera kugwiritsa ntchito Mau a Mulungu kuti alandire cholowa cha mphamvu yake.

Mpingo wayamba unagwiritsa ntchito Mau a Mulungu a mphamvu. Paulo anati:

Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'cionetso ca Mzimu ndi ca mphamvu; (1 Akorinto 2:4, 5)

Koma ndidzafika kwa inu msanga, akandilola Ambuye; ndipo ndidzazindikira si mau a iwo odzitukumula, koma mphamvuyi. (1 Akorinto 4:19)

MPHAMVU YA MAU

Mulungu nde mphamvu imene iri kumbuyo kwa Mau Ake:

Ndipo Yehova anati kwa ine, Waona bwino pakuti Ine ndidzadikira mau anga kuwacita. (Yeremiya 1:12)

Mau a Mulungu amapereka mphamvu ya Uzimu yayikulu:

mphepo yolimba yocokera kumeneko idzandifika ine; tsopanonso ndidzaweruza iwo maweruzo. Ahebri 4:12

Mulungu amalemekeza Mau Ake Padzina Lake:

Ndidzagwadira kuloza ku Kacisi wanu woyera, Ndi kuyamika dzina lanu, Cifukwa ca cifundo canu ndi coonadi canu; Popeza munakuzitsa mau anu koposa dzina lanu lonse. (Salimo 138:2)

Ndizolinga ziti zamphamvu zimene zinakwaniritsidwa ndi Mau a Mulungu? Werengani ma vesi otsatirawa. Mau a Mulungu:

- Ndi opindulitsa pa chiphunzitso, chitsutsano, chikonzero, ndi chilangizo: 2 Timoteo 3:16
- Amabweretsa chikhulupiriro ku Uthenga Wabwino: Machitidwe 4:4
- Amayeretsa: Yohane 15:3; Aefeso 5:26
- Amabweretsa moyo wosatha, ngati timva ndikuwakhulupirira: Yohane 5:24
- Ndi maziko achiweruzo chamuyaya: Yohane 12:48
- Amagwiritsidwa ntchito potulutsa mizimu yoipa: Mateyu 8:16; Luka 4:36
- Amatsatana ndi zizindikiro zozizwa ndipo amabweretsa anthu kuchowonadi cha Uthenga Wabwino: Marko 16:20
- Amapereka chitsimikizo cha chipulumutso: 1 Yohane 1:2-6
- Amabweretsa kutembenuka mtima: 1 Petro 1:23; Masalimo 119:41
- Amayeretsa okhulupirira : 1 Timoteo 4:5
- Amapereka chiyembekezo: Masalimo 130:5; 119:49, 81

- Amabweretsa machititso: Masalimo 107:20
- Amatiteteza ife kuntchito yachiwonongeko: Masalimo 17:4
- Ndi mzimu ndi moyo: Yohane 6:63
- Amabweretsa chimwemwe ndi kukondwa: yeremiya 15:16
- Amakulitsa chikhulupiriro : Aroma 10:17
- Amatonthoza: 1 Atesalonika 4:18; Masalimo 119:50,52
- Amabweretsa thanzi la uzimu: 1 Timoteo 4:6
- Amabweretsa yankho kumapephero : Yohane 15: 7
- Ndi chifungulo chachipambano: Yoswa 1:8
- Amadalitsa,ngati tiwamva ndi kuwasunga: Luka 11: 28
- Amabweretsa madalitso ngati tiwasunga ndi temberero ngati sitiwasunga:
Deutoronomo 28
- Ndi chida mu nthawi yamayesero: Mateyu 4
- Amatembenusa moyo: Masalimo 19:7
- Amapereka kuwala: 19: 8
- Amachenjeza: Masalimo 19:11
- Amapereka mwayi wokalowa kumwamba: Chibvumbulutso 22:14
- Amabweretsa mdalitso woyenda mchilungamo: Masalimo 119:1-3
- Amatipanga ife kukhala anzeru kuposa adani anthu, aphunzitsi ndi okalamba:
Masalimo 119:98-104
- Amapereka moyo: 119:25
- Amaperaka mphamvu: Masalimo 119:28
- Ndimaziko achifundo Chake: Masalimo 119:58
- Amabweretsa chikondwerero: Masalimo 119:98
- Amapereka kuzindikira kwa ozichepetsa: Masalimo 119:130, 104, 169

- Amalanditsa: Masalimo 119:170

UDINDO WA MAU

Chifukwa chakuti Mau a Mulungu ndi amphamvu kwambiri, okhulupirira ali ndi udindo opanga kuti mauwa adziwike. Mpingo woyamba unatenga udindo umenewu wa Mau a Mulungu.

Anapita kulikonse kulalikira (Machitidwe 8:4; 12:24; 13; 49). Anamupepha Mulungu kuti awapatsse kulimba mtima kuti akathe kuyakhula Mau Ake (Machitidwe 4:29, 31). Mau a Mulungu anachulukirachulukira pa dziko lonse chifukwa cha kukhulupirika kwao (Machitidwe 6:7; 19:20)

Mulungu anatsimikiza Mau Ake ndi zizindikiro zomwe zinatsatira. Wina sangadikire zizindikiro zomwe zimabwera ndi Mau. Muli ndi udindo ofalitsa Mau amphamvu amenewa ku dziko lonse.

Phunzirani za udindo wanu powerenga malemba otsatirawa:

- Mulungu amaika Mau Ake mwa inu kuti muyakhule kwa ena: Deuteronomo:18:18-19; Yesaya 51:16; Yeremiya 1:9; 3:12; 5:14; 26:12; Ezekiele 2:7-8.
- Ngati mwaphunzitsidwa mu Mau a Mulungu, nde kuti muli ndi udindo okaphunzitsaso ena: Agalatiya 6:6.
- Mukuyenera kulakira Mau ku dziko lonse lapansi: Luka 24:47; Marko 16:15; 2 Timoteo 4:2.
- Simukuyenera kuyakhula mau anu, koma Mau Ake: Yesaya 58:13.
- Simukuyenera kuchita manyazi ndi Mau Ake: Marko 8:38.
- Mukuyenera kuwaphunzitsa ana anu Mauwa: Deuteronomo 6:6-9

MAU AYINU MWINI

Malemba Oyera alindi mphamvu yakumwamba chifukwa ndi Mau a Mulungu wamoyo ndi wowona. Koma mau ayinu mwini ndi amphamvunso, makamaka pamene muyakhula Mau a Mulungu. Mukhoza kumugonjetsa satana kupyolera mu mau.

Ndipo iwo anamlaka iye cifukwa ca mwazi wa Mwanawankhosa, ndi cifukwa ca mau a umboni wao; ndipo sanakonda moyo wao kungakhale kufikira imfa. (Chibvumbulutso 12:11)

Kumvomereza ndi pakamwa panu ndi mbali imodzi yachipulumutso:

Ndipo iwo amene ali m'thupi sangathe kukondweretsa Mulungu. Koma inu simuli m'thupi ai, koma mumzimu, ngatitu Mzimu wa Mulungu akhalabe mwa inu. Koma ngati munthu alibe Mzimu wa Kristu, siali wace wa Kristu. Ndipo ngati Kristu akhala mwa inu, thupilo ndithu liri lakufa cifukwa ca ucimo; koma mzimu uli wamoyo cifukwa ca cilungamo. (Aroma 10:8-10)

Lilime lanu lili ndi mphamvu yobweretsa imfa yauzimu kapena moyo pamene mutumikira kwa ena:

Lilime liri ndi mphamvu pa imfa ndi moyo; Wolikonda adzadya zipatso zace. (Miyambo 18:21)

Mau anu antha kukupangitsani kuti musazindikire mphamvu ya Mau a Mulungu:

Amene amati, Ndi lilime lathu tidzaposi; Milomo yathu nja ife eni; mbuye wa pa ife ndani? (Masalimo 12:4)

Satana amagwiritsa ntchito zinthu zimene mwanena kuti abweretse chisokonezo mu uzimu mwanu. Chisokonezo ndi khomo limene satana angalowere.

Kuciza lilime ndiko mtengo wa moyo; Koma likakhota liswa moyo. (Miyambo 15:4)

Zomwe mmayakhula zimawononga moyo wanu:

M'kamwa mwa wopusa mumuononga, Milomo yace ikhala msampha wa moyo wace. (Miyambo 18:7)

Miyeso yosiyana inyansa Yehova, Ndi mulingo wonyenga suli wabwino. (Miyambo 21:23)

Mau anu amadetsa thupi lanu lonse:

Ndipo lilime ndilo moto; ngati dziko la cosalungama mwa ziwalo zathu laikika lilime, ndili lodetsa thupi lonse, niliyatsa mayendedwe a cibadwidwe, ndipo liyatsidwa ndi gehena. (Yakobo 3:6)

Okhulupirira amaletsa kuyenda kwa mphamvu ya Mulungu mmoyo mwawo chifukwa cha mau awo. Amayakhula zosilira, mafano, ndi mau opanda pake. Amatsutsana pazamalamulo a anthu

amene amapotoza anthu pa chilungamo cha Uthenga Wabwino. Amayakhula mau oipa kwa ena, amang'ung'udza, amadandaula, amazikweza, ndiposo amayakhula bodza. Amayakhula mau amene amabweretsa kugawanikana, mau otemberera ndiposo owawa.

Kenako amadabwa kuti nchifukwa chiyani ali opanda mphamvu.

Kumbukirani: Kuyenda kwa mphamvu ya Mulungu moyo mwanu sikumakhudzidwa ndi Mau a Mulungu okha.

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani Vesi yotsogolera osawonera.

2. Kodi ndi kwandani kumene kumachokera mau a mphamvu?

3. Kodi mau oti “rhema” amatanthauza chiyani?

4. Kodi mau oti “logos” amatanthauza chiyani?

5. Kodi Yesu anakumana bwanji ndi mayesero a satana?

6. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira mu phunziroli zokhudzana ndi udindo wanu ku Mau a mphamvu a Mulungu.

7. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira muphunziroli zokhudzana zolinga zamphamvu ya Mau a Mulungu.

8. Kodi kunena uku mkuwona kapena konama? “Mau anu alibe mphamvu yosokoneza mphamvu ya uzimu.”

Kunenaku ndi_____.

(Mayankho amafusowa apekeredwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Weremgani Genesis chaputala 1. Onani mphamvu yolenga Mau a Mulungu. Tsekani mzere kungsi kwa mau “ndipo Mulungu anati.”
2. Phunzirani zambiri zokhudzana ndi mphamvu ya lilime lanu mu phunziro la sukulu ya Harvestime International “*Ndondomeko za Uzimu: Buku la Nkhondo ya Uzimu.*” Ndondomeko zo tetezera lilime lanu zaperekedwa mu buku limeneri.
3. Yesu ankatchulidwa kuti Mau a Mulungu mumawonekedwe a umunthu. Werengani Yohane 1.
4. Kulembedwa koyamba kwa Mau a Mulungu ndi munthu kukupezeka mu Eksodo 20:1-17.
5. Pali magawo awiri a Mau a Mulungu. Mkaka wa Mau ndi nyama ya Mau. Mkaka wa Mau ndi chowonadi chimene chili chosavuta kuchimvetsa. Nyama ya mau ndi chiphunzitso chakuya cha Mau a Mulungu chimene chimabweretsa kukula kwa uzimu. Werengani zamaguluwa mu Ahebri 5:13-14 ndi 1 Petro 2:2.

CHAPUTALA 15

NDONDOMEKO YA MPHAMVU 9:

MPHAMVU YA ULAMULIRO

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osawonera.
- Kufotokoza chifukwa chimene mukuyenera kukhalalira pansi pa ulamuliro nd icholinga choti mukathe kugwiritso ntchito ulamuliro.
- Kufotokoza mmene Yesu analiri munthu wa ulamuliro pansi pa ulamuliro.
- Kulozera ndondomeko za ulamuliro zimene Mulungu anakhazikitsa mu mpingo.
- Kulozera ndondomeko za ulamuliro zimene Mulungu anakhazikitsa mmakomo.
- Kufotokoza ndondomeko za ulamuliro zimene Mulungu anakhazikitsa maubwezi ndi pa ntchito.
- Kupereka umboni umene umafotokoza zagwirizano wa okhulupirira ndi ulamuliro wa boma.

VESI YOTSOGOLERA:

Anthu onse amvere maulamuliro a akulu; pakuti palibe ulamuliro wina komawochokera kwa Mulungu; ndipo iwo amene alipo aikidwa ndi Mulungu. (Aroma 13:1

MAU OYAMBA

Kuchokera ku Mau akulenga, Mulungu wakhala akugwira ntchito pofuna kubweretsa mtendere kuchisokonezo. Mwanjira ina imene Wachitira izi ndi kukhazikitsa ndondomeko ya ulamuliro mbali zonse za moyo. Olamula wamkulu ndiye Mulungu Mwini, Mwana Yesu Kristu, ndi Mzimu Woyera.

Mulungu anakhazikitsanso ndondomeko ya ulamuliro imene imakhudza moyo wanu. Maulamuliro amanewa ndi ofunika kwambiri ngati mukufuna mphamvu ya uzimu.

MUNTHU PANSI PA ULAMULIRO

Tsiku lina ku Kaperna, Yesu anakumana ndi mtsogoleri wankhondo. Dzina la mtsogoleriyu silinaperekedwe. Tangouzidwa kuti anali Kenturiyo ndipo anali ndi wantchito amena amadwala. Werengani nkhani ya Kenturiyo pa Mateyu 8:5-13 ndi Luka7:1-10 musanapitirire ndi phunziroli.

Kenturiyo anali munthu amene anali pansi pa ulamuliro wa Aroma. Iyenso anali ndi ulamuliro, monga anali mtsogoleri wagulu la nkondo la anthu 100. Chifukwa chachimenechi anamvetsa mwachangu ngwirizano umene Yesu anali nawo ndi Atate umene Unali chimodzi modzi ndi ubale umene iye analinawo monga Kenturiyo ndi omutsogolera wake.

Yesu anali munthu waulamuliro. Anachita mwaulamuli. Anakhulukira machimo, anachiritsa odwala, anatulutsa ziwanda, ndiposo anachita zozizwa. Koma yesu anali pansi pa ulamuliro. Anali pansi pa ulamuliro wa Atate Ake.

Pamenepo Yesu anayankha nati kwa iwo, Indetu, indetu, ndinena kwa inu, sakhoza Mwana kucita kanthu pa yekha, koma cimene aona Atate acicita, ndico. Pakuti zimene iye azicita, zomwezo Mwananso azicita momwemo. (Yohane 5:19)

Pakuti monga Atate ali ndi moyo mwa iye yekha, momwemonso anapatsa kwa Mwana kukhala ndi moyo mwa iye yekha; ndipo anampatsa iye mphamvu ya kucita mlandu, pakuti ali Mwana wa munthu. (Yohane 5:26-27)

Pakuti ndinatsika Kumwamba, si kuti ndicite cifuniro canga, koma cifuniro ca iye amene anandituma Ine. (Yohane 6:38)

Pamenepo Yesu anayankha iwo, nati, Ciphunzitso canga siciri canga, koma ca iye amene anandituma Ine. (Yohane 7:16)

(Yohane 8:29)

Kenturiyo anazindikira mphamvu ya ulamuliro ya ndondomeko imeneyi ndipo, chifukwa cha ichi, anadziwa kuti kunali kosafunikira kuti Yesu achite kupita kunyumba kwake kukamuchiritsa wa ntchito wake. Anadziwa kiuti Yesu anali ndi mphamvu zongoyakhula mau ndipo machiritso abwera. Yesu anamuyamikira Kenturiyo chifukwa chachikhulupiro chake ndipo anamuchiritsa wantchito wake.

Kulikonse kumene ulamuliro ukuwonetsedwera, pamakhala ndandanda wa ulamuliro. Ichi ndi chifukwa chake Alembi ndi Afalisi anamufusa Yesu “Muchita izi ndi ulamuliro wotani?” (Mateyu 21:23). Pamene anthu awona miyoyo ikudzadzidwa ndi mphamvu ndi ulamuliro, amafuna kuti adziwe komwe zikuchokera.

YESU PANSI PA ULAMULIRO

Mulungu analingalira za wina yemwe angapite ndi ulamuliro Wake:

Ndipo ndinamva mau a Ambuye akuti, Ndidzatumiza yani, ndipo ndani adzatimukira ife? Ndipo ine ndinati, Ndine pano; munditumize ine. (Yesaya 6:8)

Mulungu anapereka mulingo wa ulamuliro Wake kwa amuna ndi akazi mu Chipangano Chakale, koma bvumbulutso lake lonse la mphamvu ndi ulamuliro Wake inabwera ndi Yesu Kristu. Yesu amkadziwa kuti analindi ulamuliro wu:

Ndipo Yesu, poona makamu ambiri a anthu akumzungulira Iye, analamulira ophunzira amuke ku tsidya lina, (Mateyu 28:18)

Yesu anawonetsera ulamuliro umene anali nawo:

Koma kuti mudziwe kuti ali nazo mphamvu Mwana wa munthu pansi pano za kukhululukira macimo (pomwepo ananena kwa wodwalayo), Tanyamuka, nutenge chika lako, numuke kunyumba kwako. (Mateyu 9:6)

Yesu analandira ulamuliro wake kuchokera kwa Mulungu ndipo chifukwa cha ichi anakwanitsa kupambana mphamvu za mdani.

Yesu ndi mutu wa maukulu ndi mphamvu zonse (Akolose 2:10) chifukwa...

atabvula maukulu ndi maulamuliro, anawaonetsera poyera, nawagonjetsera nako. (Akolose 2:15)

Yesu anali ndi ulamuliro wa Mulungu komanso ulamuliro pa mphamvu ndi maulamuliro onse. Monga mmene mwaphunzirira kale mbuyomu, Yesu anapereka ulamuliro kwa inu.

Monga ngati munthu wa paulendo, adacoka kunyumba kwace, nawapatsa akapolo ace ulamuliro, kwa munthu ali yense nchito yace, nalamulira wapakhomo adikire. (Marko 13:34)

Muli pansi pa ulamuliro wa Yesu ndipo, pochita choncho mumakhalanso pansi pa ulamuliro wa Atate. Okhulupirira ndi anthu amene ali ndi ulamuliro wauzimu.

MAULAMULIRO OIKIDWA NDI MULUNGU

Mwaphunzira kale kuti Mulungu ndiye chiyambi cha mphamvu:

pakuti mwa iye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando yacifumu, kapena maufumu, kapena maukulu, kapena maulamuliro; zinthu zonse zinalengedwa mwa iye ndi kwa iye. (Akolose 1:16)

Mulungu ndiye mphamvu zomwe ziri kumbuyo kwa ndondomeko ya ulamuliro imene anakhazikitsa m'dziko.

Anthu onse amvere maulamuliro a akulu; pakuti palibe ulamuliro wina koma wocokera kwa Mulungu; ndipo iwo amene alipo aikidwa ndi Mulungu. (Aroma 13:1)

Pamene muli pansi pa ulamuliro, mumakhala ndi kodalirika kumen ulamuliro wanu umachokera. Mwachitsanzo, mkazi panyumba amatenga ulamuliro kwamamuna wake. Akulu ampingo mu mpingo amatenga ulamuliro wawo kuchokera kwa anthu a Mulungu amene utsogoleri wa uzimu unaikidwa pa iwo. Olembedwa ntchito ali ndi malire a ulamuliro umene unaikidwa ndi olemba ntchito. Koma ndandanda onsewu umamatsogolera mwachindunji kwa Mulungu, amene ndi kochokera ulamuliro onse.

Ma ulamuliro onse amakhazikitsidwa ndi Mulungu. Tikamawafufuza maulamuliro onse kumene amachokera, nthawi zonse timamalizira kwa Mulungu. Pamene mwaukira amene ali mu ulamuliro mumakhala kuti mukuukira Mulungu.

Anthu onse amvere maulamuliro a akulu; pakuti palibe ulamuliro wina koma wocokera kwa Mulungu; ndipo iwo amene alipo aikidwa ndi Mulungu. Kotero kuti iye amene atsutsana nao ulamuliro, akaniza coikika ndi Mulungu; ndipo iwo akukaniza, adzadzitengera kulanga (Aroma 13:1-2)

Kukhala munthu wa ulamuliro, mukuyenera kukhala pansi pa ulamuliro wa Mulungu ndi wa onse amene Mulungu anawaika pamwamba panu. Uwu ndi ndandanda umene Mulungu anakhazikitsa.

MAULAMULIRO A PANYUMBA

Ndandanda weniweni woyamba umene Mulungu anakhazikitsa unali nyumba (Genesis 1-3).

Uwu ndi ndandanda wa Mulungu wapanyumba:

AMUNA:

Baibulo limaphunizitsa kuti mamuna akuyenera kukhala mutu wa pakhomo. Ulamuliro wa panyumba ukuyenera kukhazikika pa chikondi:

Pakuti mwamuna ndiye mutu wa mkazi, monganso Kristu ndiye mutu wa Eklesia, ali yekha Mpulumutsi wa thupilo. Amuna inu, kondani akazi anu, monganso Kristu anakonda Eklesia, nadzipereka yekha m'malo mwace; (Aefeso 5:23, 25)

AKAZI:

Mkazi akuyenera kukhala pansu pa ulamuliro wachikondi cha mamuna wake.

Amuna inu, kondani akazi anu, monganso Kristu anakonda Eklesia, nadzipereka yekha m'malo mwace; (Aefeso 5:22)

MAKOLO:

Pamodzi, mkazi ndi mamuna a kuyenera kukhala ndi ulamuliro pa ana awo:

Ananu, mverani akukubalani mwa Ambuye, pakuti ici ncabwino. Lemekeza atate wako ndi amako (ndilo lamulo loyamba lokhala nalo lonjezano), kuti kukhale bwino ndi iwe, ndi kuti ukhale wa nthawi yaikuru padziko. (Aefeso 6:1-3)

Koma makolo anachenjedwa:

Ndipo atate inu, musakwiyitse ana anu; komatu muwalere iwo m'maleredwe ndi cilangizo ca Ambuye. (Aefeso 6:4)

Ulamuliro umayenda limodzi ndi udindo. Makolo akuyenera kugwiritsa ntchito ndi ulamuliro wawo mwaumulungu ndi chikondi. Amuna akuyenera kugwiritsa ntchito utsogoleri umene ngati wa Kristu kwa mpingo. Sakuyenera kukhala ngati bwana ndi amwano ndi kumafuna kuti mkazi ndi ana azimutumikira iwo ngati akapolo. Akuyenera kuyanjana ndi banja lawo ngati mmene Yesu amachitira ndi Mpingo.

Amuna akuyenera kumvera akazi awo, monga ali mphatso yochokera kwa Mulungu ndi “othangatira.” Mkazi angathangatiye bwanji mamuna amene samvera mkazi wake komaso amanyoza maganizo ake? Pali zimene zinalembedwa m’Baibulo pamene Mulungu anawauza amuna kuti azimvera akazi awo (Abrahamu) Mulungu anayakhula ndi mkazi koyamaba asanayakhule ndi mamuna (Manowa). Ichi nchifukwa chake kuli kofunika kuti mamuna ndi mkazi akuyenera kumayakhana bwino wina ndi nzake.

Ndondomeneko iriyonse ya ulamuliro ikuyenera kukhala yabwino ndi yokonedwa. Koma mwatsoka, ulamuliro wagwiritsidwitsidwa ntchito molakwika ndipo anthu nthawi ambiri saugwiritsanso ntchito mu njira ya chikondi ndi moyenera. Ngati nyumba iribe mtenderere, munthu sangathe kugwira ntchito yautsogoleri yake bwino bwino mu utumiki omwe uli udindo waukulu. Ichi ndi chifukwa chake Mulungu anakhazikitsa udindo waulamuro pa nyumba monga choyenera cha utsogoleri wa mpingo.

kuyenera woyang'anira akhale wopanda cirema, mwamuna wa mkazi mmodzi, wodziunga, wodziletsa, wolongosoka, wokonda kucereza alendo, wokhoza kuphunzitsa; woweruza bwino nyumba yace ya iye yekha, wakukhala nao ana ace omvera iye ndi kulemekezeka konse. Asakhale wophunza, kuti podzitukumula ungamwere mlandu wa mdierekezi. (1 Timoteo 3:2, 4-5)

ngati wina ali wopanda cirema, mwamuna wa mkazi mmodzi, wokhala nao ana okhulupirira, wosakaza zace, kapena wosakana kumvera mau. (Tito 1:6)

Baibulo laimayakhulaso zoti mapemphero amatchingidwa pamene pali kusagwirizana pakati pa mamuna ndi mkazi.

ULAMULIRO MU MPINGO

Pamene tikuyakhula za ulamuliro wa mu Tchalitchi, sitikuyakhula za dongodolo la munthu. Tikukamba za ndondomeko imene Baibulo limakamba imene inakhazikitsidwa ndi Mulungu. Mutu wa Mpingo ndi Yesu Kristu ndipo okhulupirira ndi...

Koma inundinu thupi la Kristu, ndi ziwalo, yense pa yekha. (1 Akorinto 12:27)

Mulungu anakhazikitsa mu mpingo mphatso zapaderadera:

Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; (Aefeso 4:11)

Mphatso za utsogolerezi zinaikidwa mu mpino ndi Mulungu. Pamene mwakhala mbali imodzi ya mpingo wapamalo, pamene mwakhala pansi pa ulamuliro wa anthu amene Mulungu wawaika ngati atsogoleri, atsogoleri apaderadera amathandizidwa ndi akulu ampingo amene amayenera kutumikira pansi pa utsogoleri wawo. Mukhoza kuwerenga zokhudzana ntchito ndi zowayenereza amuna amenewa mu 1 Timeteo 3 ndi Tito 1.

Mulungu anaperekaso mphatso ya uzimu kwa okhulupirira aliyense amene anadzadidwa ndi Mzimu. Mphatso zimenezi zikuyenera kugwira ntchito mu mpingo pansi pa ulamuliro wa utsogoleri ndi zolinga zomangilira ntchito ya utumiki. Mukhoza kuwerenga za mphatso mu ndime zotsatirazi: Aroma 12:1-8; 1 Akorinto 12:1-3; Aefeso 4:1-16; 1 Petro 4:1-11. Mukhoza kuphunzira za mphatso zapaderadera mwatsanetsatane mu phunziro la sukulu ya Harvestime International lotchedwa, *“Utumiki wa Mzimu Woyera.”*

Mpingo ndi thupi la Yesu Kristu la uzimu. Aliyense wa mu mpingo ali ndi udindo wosiyana ndi mzake, monga mmene ziriri ziwalo za thupi la munthu. Chiwalo chirichonse chimaloza mbali imene kuli mutu wa mpingo, Yesu Kristu.

Muthupi la munthu, chiwalo chirichonse chimalandira chitsogozo kuchokera kumutu. Zironso chimodzimodzi mu thupi lauzimu la mpingo. Pakhoza kukhala kusagwirizana m’thupi popanda ulamuliro wa mutu, Yesu Kristu.

Okhala m’thupi akuyenera kumazipereka kwa wina ndi nzake, monga momwe zimakhallira kuthupi la umunthu. Mwachitsanzo, ikafika nthawi yowerenga, maso amatenga ulamuliro. Pamene yafika nthawi yoyenda, mapazi amatenga ulamuliro. Okhala munthupi la uzimu akuyenera kuziperekaso chimodzimodzi kuti pakakhale kugwira ntchito mopambana mu utumiki.

MAULAMULIRO PA NTCHITO:

Baibulo linakhazikitsa ndondomeko ya ulamuliro kwa onse amene akugwira ntchito kaya ndi wolembedwa kapena olemba. Wolemba ntchito ndi amene ali mtsogoleri, bwana, kapane amene ali ndi ulamuliro pa ogwira ntchito. Olembedwa ntchito ndi amene walembedwa ndipo ali ndi udindo wa ogwira ntchito.

Baibulo limaphunzitsa:

Akapolo inu, mverani iwo amene ali ambuye anu monga mwa thupi, ndi kuwaopa ndi kunthunthumira nao, ndi mtima wanu wosakumbukila kanthu kena, monga kwa Kristu; podziwa kuti cinthu cokoma ciri conse yense acicita, adzambwezera comweci Ambuye, angakhale ali kapolo kapena mfulu. (Aefeso 6:5-8)

Wolembedwa ntchito akuyenera kugwirira kwa Atate chifukwa Mulungu ndiye kochokera mphamvu zonse. Malanginzo anaperekedwaso kwa olemba ntchito. Ndongomeko ya amene ali panso pa ulamuliro yawonetseredwaso mu ndime iyi:

Ndipo, ambuye inu, muwacitire zomwezo iwowa, nimuleke kuwaopsa; podziwa kuti Ambuye wao ndi wanu ali m'Mwamba, ndipo palibe tsankhu kwa iye. (Aefeso 6:9)

Olemba ntchito akuyenera kuwasamala antchito awo bwinobwino, monga ngati iwo mmene amasamalidwira bwino ndi Mulungu kumene iwo amatengako mphamvu zao.

MPHAMVU M'BOMA:

Malingana ndi Mateyu 20:25-28 ndondomeko ya mphamvu za dziko si yofanana ndi ya ufumu wa Mulungu. Koma ngakhale zirichoncho ife okhulupirira ndi mbali imodzi ya ufumu wa Mulungu, koma pakanali pano tikukhala mudziko lapansi. Wina aliyense wa ife amakhala kumudzi kapena mu mzinda umene ndi mbali imodzi ya dziko lalikulu, dera kapenaso dziko. Wina aliyese wa ife amakhala panso pa boma laling'ono kapena lalikulu.

Mbuyomu mwaphunzira kuti Baibulo limaphunzitsa kuti Mulungu nde chiyambi cha mphamvu zonse. Aroma 13 amafotokoza mmene izi zimagwirizanirana ndi maulamuliro a boma. Tsegulani chaputala chimenechi m'Baibulo lanu.

Vesi 1 ikuphunzitsani kuti Mulungu nde kochokera mphamvu zonse nde aliyense akuyenera amvere onse amene akulamulirani.

Vesi 2 ikuwonetsa kuti pamene mwaukira onse amene akulamulira, mumakhala mukuukira Mulungu.

Vesi 3 ndi **4** akufotokoza kuti otsogolera a boma ndi oopsa kwa inu pamene simukuwamvera iwo. Akufaniziridwa ndi atumiki a Mulungu.

Mulungu amaika atsogoleri aboma ndi mphamvu ndipo amathanso kuwachotsa pampano:

pakuti amasanduliza nthawi ndi nyengo, acotsa mafumu, nalonga mafumu, apatsa anzeru nzeru, ndi cidziwitso kwa iwo okhoza kuzindikira. (Danielo 2:21)

(Danieli 4:17)

Danielo akunena nkhani ya mfumu yotchedwa Nebukatineza amene samazindikira kochokera mphamvu za dziko la pansi kufikira pamene Mulungu anamuphunzitsa iye:

Koma pokwezeka mtima wace, nulimba mzimu wace kucita modzikuza, anamtsitsa pa mpando wa ufumu wace, namcotsera ulemerero wace; ndipo anamuinga kumcotsa kwa ana a anthu, ndi mtima wace unasandulika ngati wa nyama za kuthengo, ndi pokhala pace mpa mbidzi, anamdyetsa udzu ngati ng'ombe, ndi thupi lace linakhathamira ndi mame a kumwamba; mpaka anadziwa kuti Wam'mwambamwamba alamulira m'ufumu wa anthu, nauikira ali yense Iye afuna mwini. (Danielo 5:20-21)

Mulungu anatumiza mneneri kwa mfumu Amaziya kukamulangiza pamene amakozekera nkhondo:

Koma anamdzera munthu wa Mulungu, kuti, Mfumu, khamu la nkhondo la Israyeli lisapite nanu; pakuti Yehova sakhala ndi Israyeli, sakhala ndi ana onse a Efraimu. Koma ngati mumuka, citani, limbikani kunkhondo, Mulungu adzakugwetsani pamaso pa adani; pakuti Mulungu ali nayo mphamvu yakuthandiza ndi yakugwetsa. (2 Mbiri 25:7-8)

Ma vesi amenewa akuwonetsa poyera kuti Mulungu ndi amene amaika olamulira a boma Atsogoleri oipa ndi amwano olanda ulamulira mmaiko ambiri amakana kuzindikira Mulungu ngati kochokera mphamvu ndipo amabweretsa chizuso kwa okhulupirira. Pamene boma likutsutsana ndi zimene zanededwa M'mau a Mulungu, mukuyenera kumvera Mulungu kusiyana kumvera munthu. Pamene ophunzira anauzidwa kuti asalalikire mu dzina la Yesu...

Ndipo anayankha Petro ndi atumwi, nati, Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu. (Machitidwe 5:29)

Anazindikira kuti pempho limeneri likusemphana ndi lamulo la Yesu lomwe anawauza kuti akalalikire Uthenga Wabwino pa dziko lonse lapansi. Nthawi zina mukuyenera ku...

Cifukwa cace, kuyenera kuti mukhale omvera, si cifukwa ca mkwiyo woo kha, komanso cifukwa ca cikumbu mtima. Pakuti cifukwa ca ici mupatsanso msonkho; pakuti iwo ndi wo atumiki a Mulungu akulabadira be cinthu cimeneci. Perekani kwa anthu onse mangawa ao; msonkho kwa eni ace a msonkho; kuli pira kwa eni ace a kulipidwa; kuopa kwa eni ace a kuwaopa; ulemu kwe eni ace a ulemu. (Aroma 13:5-7)

Chifukwa cha udindo waukulu ndi kuthekera kwawo kogwiritsa udyo mphamvu zawo, mukuyenera kupemphera...

cifukwa ca mafumu ndi onse akucita ulamuliro kuti m'moyo mwathu tikakhale odika mtima, ndi acete m'kulemekeza Mulungu, ndi m'kulemekezeka monse. (1 Timoteo 2:2)

MPHAMVU ZONSE ZIMAKHALA MPHAMVU ZA MULUNGU

Mulungu ndi kochokera mphamvu zonse za dziko la kuthupi ndi lauzimu. Mphamvu zonse zimaperkedwa ndi Iye. Koma ikudza nthawi mtsodolomu pamene mphamvu zonse zoperekedwa zizabwerereso ku mphamvu Zake:

Pomwepo pali cimariziro, pamene adzapereka ufumu kwa Mulungu, ndiye Atate, atatha kuthera ciweruzo conse, ndi ulamuliro wonse, ndi mphamvu yomwe. (1 Akorinto 15:24)

Ndipo pamene zonsezo: zagonjetsedwa kwa iye, pomwepo Mwana yemwe adzagonjetsedwa kwa iye amene anamgonjetsera zinthuzonse; kuti Mulungu akhale zonse mu zonse. (1 Akorinto 15:28)

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani Vesi yotsogolera osawonera.

2. Nchifukwa chiyani mukuyenera kukhala pansu pa ulamuliro kuti mukathe kugwiritsa ntchito ulamuliro?

3. Fotokozani mmene Yesu analiri ndi ulamuliro pansu pa ulamuliro.

4. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira zokhudzana ndondomeko ya ulamuliro imene Mulungu anakhazikitsidwa mu mpingo.

5. Fotokozani za ndondomeko ya ulamuliro yomwe Mulungu anakhazikitsa mmalo ogwirako ntchito.

6. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira za ndondomeko ya ulamuliro imene Mulungu anakhazikitsa pa nyumba.

7. Perekani umboni wa m'Baibulo umene umafotokoza zaubale wa okhulupirira ndi kwa olamulira boma.

8. Pamene mwaukira ulamuliro umene uli pamwamba panu, kodi kweni kweni makhala mukuukira ndani?

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Werengani Machitidwe 6:1-6 pachitsanzo cha ulamuliro umene ukugwira ntchito mu ndondomeko ya Mpingo. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira zokhudzana ulamuliro kuchokera mu ndime imeneyi.
-
-

2. Mu Afilipi 4:2 Paulo anapempha kuti mtendere ukhazikitsidwe pakati pa Euodiya ndi Suntuke. Sitinauzidwe zomwe amkalimbirana, koma pamene pali vuto lotere wina samazipereka bwino bwino ku ulamuliro.

3. Werengani 1 Samuelo 13. Mu nkhani imeneyi, Mfumu Sauli anatenga ulamuliro umene sanaugwiritse bwino ntchito ngati mfumu. Anapereka msembe zomwe zimkayenera kuperekedwa ndi neneri wa Mulungu yekha basi.

Werengani 1 Samuelo 15. Apa mfumu Sauli anaukira malamulo a Mulungu potengako ng'ombe ndi mfumu Agagi kwa Amaleki.

Zotsatira za kuukira kwa mfumu Sauli zinali chani? (Onani 1 Samueli 13:13-14 ndi 15:26).

4. Werengani Yohane 19:10-11. Pirato ankayesa ngati ali ndi mphamvu pa Yesu. Kodi izi zinali zowona?
-
-

5. Lembani mwachidule malangizo amene anaperekedwa kwa amuna ndi akazi mu 1 Akorinto 7.
-
-

6. Werengani mu Machitidwe 23 mmene Paulo anaziperekera ku ulamuliro pamene anazindikira kuti munthu amene amayakhula naye anali wa msembe wa mkulu wa Mulungu. Anachitanji?
-

CHAPUTALA 16

NDONDOMEKO YA MPHAMVU 10:

MPHAMVU YA KUUKA KWAKE

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziroli mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osawonera.
- Kupereka tanthauzo lakuuka.
- Kufotokoza ubwino wa kuuka kwa Yesu.
- Kulemba mwachidule ntchito imene mphamvu ya kuuka ikugwirira ntchito kwa okhulupirira.
- Kuwonetsera komwe mphamvu ya chiukitso imachokera.

VESI YOTSOGOLERA:

Kuti ndimzindikire Iye ndi mphamvu ya kuuka kwake, ndi chiyanjano cha zowawa zake, pofaniziridwa ndi imfa yake. (Aefeso 3:10)

MAU OYAMBA

Paulo anayakhulapo za mphamvu ya uzimu imene imapezeka magawo awiri:

kuti ndimzindikire iye, ndi mphamvu ya kuuka kwace, ndi ciyanjano ca zowawa zace, pofanizidwa ndi imfa yace; (Afilipi 3:10)

Chaputala chino chakhazikika pa za mphamvu yachiukitso cha Yesu Kristu imene imakhala mwa okhulupirira. Chaputala chotsatira chikukhudzana ndi mphamvu ya chiyanjano mazuzo Ake. Palibe phunziro limene satana amadana nalo kuposa chiukitso cha Yesu, popeza limawonetsa kulephera kwake kogonjetsa dongosolo la Mulungu kuposera zonse zochitika zimene Baibulo linalimba.

TANTHAUZO LA KUUKA

Tanthauzo la mau oti “kuuka” ndi kudzuka kwa akufa kukhalanso ndi moyo.

KUUKA KWA YESU KRISTU

Potsatira imfa Yake chifukwa chamachimo a anthu onse, Yesu anaukitsidwa kwa akufa ndi Mulungu.

Macitidwe 3:15 ndipo munamupha Mkulu wa moyo; amene Mulungu anamuukitsa kwa akufa; za ici ife tiri mboni. (Machitidwe 3:15)

popeza munaikidwa m'manda pamodzi ndi iye muubatizo, momwemonso munaukitsidwa pamodzindi iye m'cikhulupiriro ca macitidwe a Mulungu, amene anamuukitsa iye kwa akufa. (Akolose 2:12)

cifukwa ca inu amene mwa rye mukhulupirira Mulungu 4 wakwnuukitsa iye kwa akufa, ndi kumpatsa iye ulemerero; kotero kuti cikhulupiriro canu ndi ciyembekezo canu cikhale pa Mulungu. (1 Petro 1:21)

Mukhoza kuwerenga nkhani ya kuuka kwa Yesu mu Mateyu 28, Marko 16, Luka 24, ndi Yohane 20.

KUFUNIKWA KWA KUUKA KWA YESU

Kuuka kwa Yesu ndi chowonadi champhamvu chifukwa ndi maziko enieni achikhulupiriro chathu:

Koma ngati kulibe kuuka kwa akufa, Kristunso sanaukitsidwa; ndipo ngati Kristu sanaukitsidwakulalikira kwathu kuli cabe, cikhulupiriro canunso ciri cabe. (1 Akorinto 15:13-14)

Kukhulupirira kuuka kwa Yesu ndikofunika pa chipulumutso:

kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka: (Aroma 10:9)

Kuukitsidwa kwa Yesu kumatsimikiza kuti okhulupirira ndi olungamitsidwa:

amene anaperekedwa cifukwa ca zolakwazathu, naukitsidwa cifukwa ca kutiyesa ife olungama. (Aroma 4:25)

Chiukitso chimatanthauza kuti imfa inagonjetsedwa:

Popeza tsono ana ndiwo a mwazi ndi nyama, Iyenso momwemo adalawa nao makhalidwe omwewo kuti mwa imfa akamuononge iye amene anali nayo mphamvu ya imfa, ndiye mdierekezi; (Ahebri 2:14)

Kuukitsidwa kwa Yesu kumatsimikiza kuti Iye ndi wamkulu kuposa cholengedwa china chirichonse:

Pakuti ndidziwa kuti ici cidzandicitira ine cipulumutso, mwa pembedzero lanu ndi mwa kundipatsako kwa Mzimu wa Yesu Kristu; monga mwa kulingiriritsa ndi ciyembekezo canga, kuti palibe cinthu cidzandicititsa manyazi, komatu mwa kulimbika mtima konse, monga nthawi yonse, tsopanonso Kristu adzakuzidwa m'thupi langa, kapena mwamoyo, kapena mwa imfa. Pakuti kwa ine kukhala ndi moyo ndiko Kristu, ndi kufa kuli kupindula. Koma ngati kukhala ndi moyo m'thupi, ndiko cipatso ca nchito yanga, sindizindikiranso cimene ndidasankha. (Aefeso 1:19-22)

Chiukitso ndi chitsimikizo kuti Yesu analidi Mwana wa Mulungu:

amene anatsimikizidwa ndi mphamvu kuti ndiye Mwana wa Mulungu monga mwa Mzimu wa ciyero, ndi kuuka kwa akufa; ndiye Yesu Kristu Ambuye wathu; (Aroma 1:4)

CHIUKITSO CHA MTSOGOLO

Baibulo limayakhula za nthawi yamtsogolo pamene dziko lino lidzafike kumapeto. Pa nthawi imeneyo kuzakhala chiukitso kwa onse amene anamwalira. Onse amene anamwalira ali okhulupirira azaukitsidwa kupita kumoyo osatha. Onse amene anamwalira ali osakhulupirira azaukitsidwa, kuweruzidwa ndipo adzapita mkuchilango chosantha.

Mukhoza kuwerenga zakhudzana chiukitso chmtsogolo pa 1 Akorinto 6:14; 15:1-58; 1 Atesalonika 4:13-14; Yohane 5:28-29; 2 Akorinto 4:14; ndi Chibvumbulutso 20:4-6. Mukhonza kuphunzira mwatsatanetsatane za chiukitso cha mtsogolo mu phunziro la sukulu ya Harvestime International lotchedwa “*Maziko a Chikhulupiriro.*”

MPHAMVU YA CHIUKITSO PANAKALI PANO

Ndi zowona kuti tsiku lina tizaukitsidwa kwa akufa, koma mphamvu ya chiukitso sinangosungidwa kuti izagwire ntchito mtsogolo mokha. Mphamvu yake ikhoza kugwiritsidwa ntchito mwa okhulupirira pa nthawi ino. Chiukitso ndi maziko a mphamvu ya uzimu imene yaperekedwa kwa inu panopa.

CHIYEMBEKEZO CHATSOPANO:

Ndi kudzera mu mphamvu ya chiukitso imene imakupatsani chiyembekezo. Moyo wanu suzathera pa manda. Inu muli ndi moyo wamuyaya:

Wodalitsika Mulungu ndiye Atate wa Ambuye wathu Yesu Kristu, iye amene, monga mwa cifundo cace cacikuru, anatibalanso ku ciyembekezo ca moyo, mwa kuuka kwa akufa kwa Yesu Kristu; (1 Petro 1:3)

Chiyembekezo ndi mphamvu yaikulu. Popanda chiyembekezo, anthu amakhumudwa komaso amakhala ndi nkhwana. Mphamvu ya chiukitso imapangitsa kuti chiyembekezo chikhalebe chamoyo.

MOYO WATSOPANO:

Pamene mwalandira Yesu kukhala Mpulumutsi, mumaukitsidwa kuimfa ya uzimu ya tchimo ndi kulandira moyo wauzimu.

Ndipo inu, pokhala akufa m'zolakwa ndi kusadulidwa kwa thupi lanu, anakupatsani moyo pamodzi ndi iye, m'mene adatikhululukira ife zolakwa zonse; (Akolose 2:13)

Chiukitso chazimu ndichotsatira cha imfa ya tchimo. Kupyolera mumphamvu ya chiukitso mukhoza kukhala moyo watsopano. Simukhalaso moyo umene mumkakhala kale. Mumamwalira kuzinthu zoipa za dziko ndipo makhala ndi moyo mwa Yesu.

Simungakhale moyo watsopano poyesetsa panokha. Simungaukhale moyowu ndi mphamvu zanu. Mumakhala moyowu kupyolera mu mphamvu ya chiukitso:

Cotero inunso mudziwerengere inu nokha ofafa ku ucimo, koma amoyo kwa Mulungu mwa Kristu Yesu. Cifukwa cace musamalola ucimo ucite ufumu m'thupi lanu la imfa kumvera zofuna zace: ndipo musapereke ziwalo zanu kuucimo, zikhale

zida za cosalungama; koma mudzipereke inu nokha kwa Mulungu, monga amoyo ataturuka mwa akufa, ndi ziwalo zanu kwa Mulungu zikhale zida za cilungamo, Pakuti ucimo sudzacita ufumu pa inu; popeza simuli a lamulo koma a cisomo. (Aroma 6:11-14)

Kulimbana komwe kumakhala mwainu kumakhala pakati pa imfa ndi moyo komwe kukugwira ntchito mwainu. Mphamvu ya chiukitso imagonjetsa lamulo la tchimo ndipo imfa imakusiyani kuchokera kugoli la uzimu. Yesu anati:

Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka. (Yohane 10:10)

Osangoti moyo osatha okha mtsogolo, komaso moyo wochulukira panakali pano ndi wanu chifukwa cha mphamvu ya chiukitso.

MBUYE WATSOPANO:

Chiukitso chazimu chimampanga Yesu kukhala Mbuye wa moyo wanu. Malo momakhala nokha, mumakhala kuti mukutumikira Iye:

ndipo adafera onse, kuti iwo akukhala ndi moyoasakhalenso ndi moyo kwa iwo okha, koma kwa iye amene adawafera iwo, nauka. (2 Akorinto 5:15)

Mphamvu imachokera pa kumvetsetsa kwanu malo anu chifukwa chachiukitso. Simulinso kapolo wa satana.

MOYO WATSOPANO WACHOLINGA:

Moyo watsopano wacholinga umabwera chifukwa cha chiukitso cha uzimu. Malo mokhudzidwa ndi zinthu zakanthawi kochepe za dziko, monga ngati kupeza zinthu zakuthupi, tsogolo, ndi zina zambiri, mumayambano kuika chidwi pa zazinthu za muyaya:

Cifukwa cace ngati munaukitsidwa pamodzi ndi Kristu, funani zakumwamba, kumene kuli Kristu wokhala pa dzanja lamanja la Mulungu. Lingalirani zakumwamba osati za padziko ai. Pakuti munafa, ndipo moyo wanu wabisika pamodzi ndi Kristu mwa Mulungu, (Akolose 3:1-3)

Zinthu za dziko lino sizilamuliranso okhulupirira amene walandira mphamvu ya chiukitso. Zochitika za padziko sizimamugonjetsa iye. Kukumana ndi mphamvu ya chiukitso kumapereka kuwona ndi chiyembekeze chatsopano kwa iye.

KUDZUTSIDWA KWA TSOPANO:

Koma ngati Mzimu wa iye amene adaukitsa Yesu kwa akufa akhalabe mwa inu, iye amene adaukitsa Kristu Yesu kwa akufa adzapatsanso moyo matupi anu akufa, mwa Mzimu wace wakukhala mwa inu. (Aroma 8:11)

Mau oti “kudzutsidwa” akutanthauza kuti kukhalaso ndi moyo ndi kudzadzidwaso ndi moyo. Mulungu wakuukitsani kale inu ku tchimo:

Ndipo inu, anakupatsani moyo, pokhala munali akufa ndi zolakwa, ndi zocimwa zanu, (Aefeso 2:1)

Mulungu akufuna adzadze matupi anu anyama ndi mphamvu ya chiukitso.

Koma tiri naco cuma ici m'zotengera zadothi, kuti ukulu woposa wamphamvu ukhale wa Mulungu, wosacokera kwa ife; (2 Akorinto 4:7)

Ngati munalandira Yesu kukhala Mpulumutsi ndi kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera, ndiye kuti mphamvu imene inamuukitsa Yesu kwa akufa imakhalanso mwa inu. Kuyenda kwa moyo kukhoza kudzutsa inu panopa ndi mphamvu yachiukitso.

KOMWE MPHAMVU YACHIUKITSO IMACHOKERA

Mphamvu yachiukitso imene iri mwa okhulupirira imachokera kwa Yesu. Anati :

Yesu anati kwa iye, Ine ndine kuuka ndi moyo; wokhulupirira Ine, angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo; (Yohane 11:25)

Monga uliri moyo wakuthupi kuti uli ndi magari, moyo wauzimu umabweranso kudzera mu mwazi wa Yesu. Monga momwe magari amayenda mumisepha, moyo wachiukitso umayendanso mu mzimu wanu. Kodi mukuyenda mumphamvu ya chiukitso panopa Mu moyo wanu wa chikhristu tsiku ndi tsiku?

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Perekani tanthauzo la mau oti “chiukitso.”

3. Lembani mwachidule ubwino wa chiukitso cha Yesu kuchokera kwa akufa.

4. Kodi kunena uku ndi kowona kapena konama? “Mphamvu ya chiukitso adzakumane nayo ndi okhulupirira okha mtsogolo pamene adzaukitsidwa kwa akufa.” Kunenaku ndi_____.

5. Lembani mwachidule zolinga za mphamvu ya chiukitso pakanali pano mmoyo mwa okhulupirira.

6. Kodi mphamvu ya chiukitso mmoyo mwa okhulupira imachokera kwandani?

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Yesu sanapitepo kumwambo wakufa... anapita ku mwambo wachiukitso...
 - Mwana wa mzimayi waku Nayini: Luka 7:11-17
 - Mwana wa mkazi wa Yairo: Marko 5:35-43
 - Lazalo: Yohane 11:1-46
 - Iye Mwini: Mateyu 28, Marko 16, Luka 24, Yohane 20
2. Kulalikira kwa chiukitso ndi mbali imodzi yofunika ya Uthenga Wabwino. Onani Machitidwe 4:2; 17:18, 32; 1 Akorinto 15:1-8, 14, 19-22.
3. Abrahamu anakhala zaka zambiri chiukitso cha Yesu chisanafike, koma anakumana ndi mphamvu ya chiukitso. Werengani Aroma 4:16-24.
4. Elisa anali ndi mphamvu yotereyi kuti munthu wakufa amene anaponyedwa mu dzenje lake la manda zaka zambiri kutsatira imfa yake anaukitsidwa! Anali ndi mphamvu zambiri mmafupa ake(2 Mafumu 13:20-21).

CHAPUTALA 17

NDONDOMEKO YA MPHAMVU 11:

MPHAMVU YA KUZUZIKA

ZOLINGA:

Pomaliza paphunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osawonera.
- Kuwonetsera komwe mazuzo amachokera.
- Kulemba njira zisanu momwe kuzuzika kumabwerera.
- Kulemba mwachidule zolinga za kuzuzika mmoyo mwa okhulupirira.

VESI YOTSOGOLERA:

**Pakuti anapachikidwa m'ufoko, koma ali ndi moyo mu mphamvu ya Mulungu.
Pakuti ifenso tiriofoka mwa Iye, koma tidzakhala ndi moyo pamodzi ndi Iye, mu
mphamvu ya Mulungu ya kwa inu. (2 Akorinto 13:4)**

MAU OYAMBA

Chaputala chapita chija chinayamba mkambirano ndi ndondomeko ziwiri za mphamvu za Afilipi 3:10.

**kuti ndimzindikire iye, ndi mphamvu ya kuuka kwace, ndi ciyanjano ca zowawa
zace, pofanizidwa ndi imfa yace; (Afilipi 3:10)**

Chaputala 16 chimakhudzana ndi mphamvu ya chiukitso mmoyo mwa okhulupirira. Chaputala chino chikuyang'ana kwambiri pa mphamvu ya chiyanjano mazuzo. Paulo anati za Yesu:

**pakuti anapacikidwa m'ufoko, koma ali ndi moyo mu mphamvu ya Mulungu.
Pakuti ifenso tiri ofok a mwa iye, koma tidzakhala ndi moyo pamodzi ndi iye, mu
mphamvu ya Mulungu, ya kwa inu. (2 Akorinto 13:4)**

Timawona kuvutika ndi kuganiza kwa umunthu. Malingana ndi kaganizidwe ka umunthu, mtanda wa Yesu kunali kutaya moyo wofunika kwambiri. Koma mkuganiza kwa Mulungu, uku kunali kuwonetsera mphamvu zake mopambana. Kunabweretsa chipulumutso kwa munthu.

Paulo anamvetsetsa ndondomeko yofunikayi ya mphamvu yauzimu. Mphamvu ya Mulungu imawonekera nchifooko. Ichi ndi chifukwa chake ananena kuti:

Ndipo ananena kwa ine, Cisomo canga cikukwanira; pakuti mphamvu yanga ithedwa m'ufoko. Cifukwa cace makamaka ndidzadzitamandira rriokondweratu m'maufoko anga, kuti mphamvu ya Kristu ikhale pa ine. Cifukwa cace ndisangalala m'tnaufoko, m'ziwawa, m'zikakamizo, m'mazunzo, m'zipsinjiko, cifukwa ca Kristu; pakuti pamene ndifoka, pamenepo ndiri wamphamvu. (2 Akorinto 12:9-10)

Sitiwona mphamvu ndi chifooko kapena mkulephera. Awa ndi malingaliro achilendo kwa onse amene mtanda uli pakati pachikhulupiriro pawo. Yesu anakumana ndi chiukitso kutsatira chizuzo chake. Mphamvu ya chiukitso imabwera kupyolera muchiyanjano cha mazuzo Ake.

Mphamvu yeniyeni ya uzimu imawonekera osati pakusapezeka kwa kwamazuzo, mavuto ndi kuvutika, koma pakati pa zonsenzi. Mphamvu zimasitha zimene dziko limazitchula kuti zopanda zake mkukhala zofunika zimene zimawonetsera mphamvu ya Mulungu.

GWERO MAMAZUZO

Mulungu Sanalenge mazuzo. Koma chizuzo chinalowa dziko lapansi chifukwa cha tchimo la munthu limene oyambitsa wake anali Satana(Genesis3). Chifuka chakuti munthu anagonjera chiyeso cha Satana, mazuzo analowa dziko lapansi. Kotera kuti ntchimo limene linabweretsa chizuzo, chiyambi chake ndi Satana. Koma chosangalatsa kwa anthu okhulupirira ndi chakuti, Mulungu amatha kugwiritsa chizuzo chimene Satana amafuna kutiononga nacho kuti akakwaniritse malingaliro ake abwino pa ife. Mulungu anatha kusintha munthu okhudzidwa ndi chizuzo kukhala munthu ogonjetsa.

ZIFUKWA ZOKUMANIRA NDI CHIZUZO

Baibulo limakamba zambiri zokhudza chizuzo, mavuto ndi nsautso. Pofuna kufotokozera mwachidule, pali njira zisanu zimene chizuzo chikhoza kubwelera mmoyo wa munthu okhulupirira. Ndipo chizuzo chonse chimene mungakumane nacho mmoyo wanu chikhoza kubwera kudzera mu njira imodzi mwa njira zimenezi:

KUCHOKERA KWA ANTHU ENA OKUZUNGULIRANI

Mazuzo akhoza kuchokera kwa anthu amene akuzungululirani inu. Yosefe ndi chitsanzo chabwino cha izi. Ngakhale kuti panalibe chimene iye analakwitsa, iye anagulitsidwa ku ukapolo ndi abale ake, ananamiziridwa ndi mkazi wa Potifara komanso anayiwalidwa ndi anthu amene anawathandiza ali mundende.

Tsopano musaphwetekwe mtima, musadzikwiyira inu nokha, kuti munandigulitsira ine kuno, pakuti Mulungu ananditumiza ine patsogolo panu kuti ndisunge moyo. Ndipo Mulungu anatumiza ine patsogolo panu kuti ndikhazike inu mutsale m'dziko lapansi, ndi kusunga inu amoyo ndi cipulumutso cacikuru. (Genesis 45:5,7)

NYENGO ZA MOYO.

Njira yachiwiri imene mazuzo amabwelera ndi kudzera nyengo zathu zamoyo wa tsikunditsiku. Chitsanzo chabwino ndi Naomi amene anakumana ndi imfa ya mamuna wake komanso ndi ana ake. Nkhaniyi ukupezeka mu buku la Rute.

Imfa ndi mbali imodzo ya moyo wathu kufikira nthawi imene Yesu Khristu adzabwerenso kachiwiri ndikugonjetsa imfa. Imfa inalowa pa dziko lapansi chifukwa cha tchimo la munthu mmodzi. Ndipo imfa ndi chinthu chachilengedwe chimene munthu wina aliyense adzakumane nacho munthawi yoikikayo (Ahebri 9:27)

UTUMIKI WANU

Chifukwa china chikumanira ndi chizuzo ndi chifukwa kumtumikira Mulungu. Chipangano Chatsopano chimakamba za kukumana ndi Mazuzo chifukwa cha dzina la Ambuye. (Machitidwe 9:16), chifukwa cha Khristu, (Afilipi 1:11-12) chifukwa chakuchita bwino (I Petro 2:19-20; 3:17), chifukwa cha moyo wanu wangwiro (I Peter 3:14), chifukwa chakuti ndi inu okhulupirira (I Petro 4:15-16), ndi chifukwa chachifuniro cha Mulungu (I Petro 4:19).

Mtumwi Paulo ndi chitsanzo chabwino cha kukumana ndi mazuzo chifukwa cha utumiki. Anthu ena amaona ngati kukumana ndi mazuzo ndi chizindikiro cholephera komanso chopanda chikhulupiriro. Koma ngati izi zili chonchi, ndiye kuti Paulo mtumwi anali munthu olephera kwambiri mu mbiri yonse ya mpingo komanso opanda chikhulupiriro.

Mtumwi Paulo anafotokoza kuti anathodwa kwakulu komanso anakumana nd nsautso waukulu (1 Akorinto 1:8) Iye akupereka chithunzithunzi china chimene chimene sichikupereka lonjezano lina lilironse la mtendere komanso kuchita bwino. Pamene Mtumwi Paulo anaitanidwa ku utumiki, iye anauzindwa za mazuzo akulu amene adzakumane nao chifukwa cha khristu Yesu (Machitidwe 9:16)

Yankho la Paulo pankhani yamazuzo ndi lakuti kuti kwapatsidwa kwa inu kwaufulu cifukwa ca Kristu, si kukhulupirira kwa iye kokha, komatunso kumva zowawa cifukwa ca iye” (Afilipi 1:29)

Paulo sanali yenkha pa utumiki wake wachizunzo. Mpingo onse wachipanagano Chatsopano unakumananso ndi chizunzo. Pa Ahebri chaputala 11 pali mbiri ya chizunzo chimene okhulupirira anakumana nacho. Koma ambiri mwa amayi ndi abambo amenewa

anapulumsidwa ndi mphamvu ya Mulungu. zitseko zandende zinatseguka ndipo anatuluka ngati mfulu. Iwo anagamulidwa kuti aponyendwe mung'anjo zamoto koma, iwo anatuluka osakhudzidwa ndi moto.

Koma ena mwa amayi ndi abambo amene anali okhulupirira sanalanditsidwe kumazuzo awo. Iwo anazunzidwa, kumangidwa ngakhale kuphedwa kumene chifukwa cha umbono wa uthenga wabwino (Ahebri 11:36-40). Timatsindika za chikhulupiriro cha anthu amoyo, koma Mulungu amaonetseranso mphamvu yake pamene okhulupirira akumwalira. Ichi ndi chikhulupiriro chenicheni chimene chimaonekera ngakhale munyengo zoipa osangoti munyengo yabwino pamene chiomboro cha Mulungu chimaonekera.

MKHONDO YOCHOKERA KU ZINTCHITO ZA SATANA:

Mazunzo okhoza kulowanso mmoyo wanu chifukwa cha ntchito za Satana. Chitsanzo cha bwino ndi nkhani ya Yobu. Buku la Yobu likuyankha funso lakuti “ndi chifukwa chiani anthu olungama amakumana ndi mavuto”

Umboni ochokera kwa Mulungu unali oti Yobu anali munthu olungama (Yobu 1:2). Yobu sanakumane ndi mavuto chifukwa chakuti anachimwa ngati mmene anzake amafotokozerana. Iwo amakhulupirira kuti ngati Yobu angalape, ndiye kuti nyengo zake zisintha. Anzake a Yobu amatenga zinthu malingana ndi mmene amazionera iwo ngati chnoonadi chimene chimagwira ntchito pa Munthu wina aliyense. Izi zili ngati kunena kuti “chifukwa chakutu Mulungu anamasula Petro mundende, chomwechonso achita izi pamoyo wanu. Koma izi sizoonadi chifukwa anthu ambiri aphedwa ali kundende ngakhale kuti anali ndi chikhulupiriro chachikulu.

Tiyenera kusamalitsa ndi mmene timaonera mazuzo amene anthu ena akukumana nao chifukwa tikhoza kuwaganizira kuti akuzunzika chifukwa cha uchimo, kusakhulupirika kapena chifukwa cha kusakhulupirira. Baibulo limaphunzitsa kuti munthu ochimwa amakolera chivundi chifukwa chakufesa kuthupi (Agalatiya 6:8) Koma sitinganene kuti anthu olungama pamene akumana ndi zovuta ndiye kuti akukolera zimene anafesa.

Yobu sanakumane ndi mavuto chifukwa chakuti anachimwa ayi, iye anali munthu olungama. Ndipo anali Mulungu amene amachitira umboni wachiyero cha Yobu. Kunali kumwamba kokha kumene kumadziwa choyambitsa chenicheni cha mazuzo a Yobu. Nkhondo yauzimu inali ikuchitika mumtima mwake, mmaganizo ake angakhale mikudzipereka kwake kwa Mulungu.

Nkhondo yaikulu imakhala ikuchiti mdziko lauzimu chifukwa cha inu. Nkhondo imeneyi imaonekera mu nyengo zolimba za moyo wanu. Koma mfundo yaikulu yopezeka mu nkhani ya Yobu ndi yakuti paline chinthu chimene chingachitike pamoyo opanda Mulungu kudziwa. Mulungu samabweretsa chizunzo pamoyo wanu. Chizunzo chimachokera kwa Satana, koma malire ake amakhazikitsidwa ndi Mulungu.

MACHIMO ANU OMWE:

Njira yachisanu imene chizunzo chimalowera mmoyo wanu ndi chifukwa cha uchimo wanu omwe. Yona ndi chitsanzo chimodzi cha mazunzo amenewa. Chifukwa chakusamvera Mulungu, Yona anatenga njira Yosempana ndi kumene Mulungu anamuza kuti akalalikire uthenga Wabwino mu mzinda wa Nenevi. Iye anakumana ndi mphepo yamphamvu panyanja imene zotsatira zake zinali kukathera m'mimba mwasomba chifukwa chauchimo wake.

Mavuto ayenera kuonedwa ngati chenjezo kuti tiunikirensa njira zathu pamaso pa Mulungu. Chifukwa mwina ngati Yona, mukhoza kukhala kuti mukukumana ndi mavuto chifukwa cha uchimo wanu. Baibulo limaonetse kuti Mulungu amalanga iwo akusamvera mau ake. Kulanga kumatathauza kupereka mwambo, kukonza kapena chidzudzulo.

Chango ciri conse, pakucitika, sicimveka cokondwetsa, komatu cowawa; koma citatha, cipereka cipatso ca mtendere, kwa iwo ozoloweretsedwa naco, ndico ca cilungamo. (Ahebri 12:11)

Mulungu amagwiritsa ntchito mazunzo pofuna kukukonzani komanso kubwenzeretani kuchifuniro chake pamoyo wanu.

Ndisanazunzidwe ndinasokera; Koma tsopano ndisamalira mau anu. Kundikomera kuti ndinazunzidwa; Kuti ndiphunzire malemba anu. Ndidziwa kuti maweruzo anu ndiwo olungama, Yehova, Ndi kuti munandizunza ine mokhulupirika. (Masalmo 119:67,71,75)

KAONEDWE KOYENERA KAMAZUNZO

Msautso sichizindikiro chakuti mwasemphana ndi chifuniro cha Mulungu. Baibulo limafotokoza kuti nsautso wa olungama uchuluka (Salimo 34:9) Pamene mukumana ndi masautso osati chifukwa chakuti mwachimwa, muyenera kukhala ndi kaonedwe kabwino ka mazunzo anuwo. Muyeso weniwen wauzimu wani ndi mmene mumachitira mukakumana ndi nyengo za msautso.

Ukalefuka tsiku la tsoka Mphamvu yako icepa. (Miyambi 24:10)

Baibulo likuonetsa mmene muyenera kuonera zinthu pamene mwakumana ndi msautso chifukwa cha chifuniro cha Mulungu

koma akamva zowawa ngati Mkristu asacite manyazi; koma alemekeze Mulungu m'dzina ili. (1 Petro 4:16)

Muyenera kupereka moyo wanu onse kwa Mulungu pozindikira kuti Mulungu chikozero chake ndi chabwino munyengo zonse.

Koteronso iwo akumva zowawa monga mwa cifuniro ca Mulungu aike moyo wao ndi kucita zokoma m'manja a Wolenga wokhulupirika. (1 Petro 4:19)

Muyenera kukhala okondwera pamene mukumana ndi chizunzo chifukwa chachifuniro cha Mulungu.

Paulo akufotokoza kuti:

kondwerani m'ciyembekezo, pirirani m'masautso; limbikani cilimbikire m'kupemphera, (Aroma 12:12)

ndipo tigwiritsa nchito, ndi kucita ndi manja athu a ife tokha; polalatidwa tidalitsa; pozunzidwa, tipirira; (1 Akorinto 4:12)

m'zonse tidzitsimikfzira ife tokha monga atumiki a Mulungu, m'kupirira kwambiri, m'zisautso, m'zikakamizo, m'zopsinja, 2 Akorinto 6:4 koma

Potero usacite manyazi pa umboni wa Ambuye wathu, kapena pa ine wandende wace; komatu umve masautso ndi Uthenga Wabwino, monga mwa mphamvu ya Mulungu; (2 Timoteo 1:8)

kuti asasunthike wina ndi zisautso izi, pakuti mudziwa nokha kuti adatiika ife ticite izi., (1 Atesalonika 3:3)

Koma iwe, khala maso m'zonse, imva zowawa, cita nchito ya mlaliki wa Uthenga Wabwino, kwaniritsa utumiki wako. (2 Timoteo 4:5)

Okonedwa, musazizwe ndi mayesedwe amoto adakugwerani inu akhale cakukuyesani, ngati cinthu cacilendo cacitika nanu: koma popeza mulawana ndi Kristu zowawa zace, kondwerani; kutinso pa bvumbulutso la ulemerero wace mukakondwere kwakukurukuru. (1 Petro 4:12-13)

Muyenera kupirira zowawa ngati msirikali:

Umve zowawa pamodzi nane monga msilikari wabwino wa Kristu Yesu. (2 Timoteo 2:3)

Puulo akufotokozera mwachidule mmene muyenera kuchitira mukakumana ndi chizunzo:

ungakhale umunthu wathu wakunja ubvunda, wa m'kati mwathu ukonzedwa kwatsopano tsiku ndi tsiku. Pakuti cisautso cathu copepuka ca kanthawi citicitira ife kulemera koposa kwakukuru ndi kosatha kwa ulemerero; popeza sitipenyerera zinthu zooneka, koma zinthu zosaoneka; pakuti zinthu zooneka ziri za nthawi, koma zinthu zosaoneka ziri zosatha. (2 Akorinto 4:16-18)

Paulo akutenge chizunzo ngati chinthu chotitumikira. Iye akufotokoza kuti chizunzo chimatithandiza pamene maso athu alunjika pa mphoto yapachimaliziro osati pa chizunzo kapena vuto lathu.

ZOTSATIRA ZABWINO ZA CHIZUNZO

Zotsatira zabwino malinga ndi chifuniro cha Mulungu ndi izi:

CHIKHULUPIRIRO CHANI CHIMAYESEDWA:

Chilichonse mudziko lauzimu chimayesedwa. Ichi ndi chifukwa chake mphamvu yachikhulupiriro chanu iyenera kuyesedwa:

Ndipo mukamuitana ngati Alate, iye amene aweruza monga mwa nchito ya yense, wopanda tsankhu, khalani ndi mantha nthawi ya cilendo canu; (1 Petro 1:17)

chimakhala chiyeso cha chikhulupiriro chanu pamene mupemphera ngati Yesu, kuti chikho chachizunzo chimupitirire, koma mapeto ake izi osachitika. Mmaloko mwake mumakakamizidwa kumwera chikho chamazuzo. Kom kudzera muchikhukulupiro, timaphunzira kuti sizitanthauza kuti mapemphero athu samayankhidwa koma kuti samayankidwa munjira imene timayembekezera kapena timafuna.

ZIMATHANDIZA KUTI TIKATONTHONZE ATHU ENA:

Wolemekezeka Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Kristu, Atate wa zifundo ndi Mulungu wa citonthozo conse, woo titonthoza ife m'nsautso yathu yonse, kuti tidzathe ife kutonthoza iwo okhala m'nsautso iri yonse, mwa citonthozo cimene titonthozedwa naco tokha ndi Mulungu. (2 Akorinto 1:3-4)

pamene Mupereka chitonthozo cha Mulungu kwa ena:

Mwa ici limbitsani manja ogooka, ndi maondo olobodoka; ndipo lambulani miseu yolunjika yoyendamo mapazi anu, kuti cotsimphinaco cisapatulidwe m'njira, koma ciciritsidwe. (Ahebri 12:12-13)

MUMAPHUNZIRA KUSAKHULUPIRIRA INU MWINI:

Paulo akufotokoza cholinga cha chizunzo chake ku Asiya:

Pakuti sitifuna abale, kuti mukhale osadziwa za cisautso cathu tinakomana naco m'Asiya, kuti tinathodwa kwakukuru, koposa mphamvu yathu, kotero kuti tinada nkhawa ngakhale za moyo wathu; koma tokha tinakhala naco citsutso ca imfa mwa ife tokha, kuti tisalimbike pa ife tokha, koma pa Mulungu wakuukitsa akufa; (2 Akorinto 1:8-9)

Mumayamba kuzindikira kuti:

Koma tiri naco cuma ici m'zotengera zadothi, kuti ukulu woposa wamphamvu ukhale wa Mulungu, wosacokera kwa ife; (2 Akorinto 4:7)

ZIMATHANDIZA KUTI MUKUNZE MAKHALIDWE ABWINO:

Makhalidwe amenewa amakuthandizani kuti mufanizidwe ndi ndi chifaniziro cha Yesu. Ndipo ichi ndiye cholinga cha chikonzero cha Mulungu (Aroma 8:28-29; Ahebri 2:10,18)

NTCHITO ZA MULUNGU ZIMAONEKERA:

Ophunzira a Yesu anafunsa kuti anachimwa ndi ndani ataona munthu wakhungu chibadwireni chake. Iwo anafunsa kuti kodi ndi makolo ake a munthuyo kapena amene anachimwa? Koma Yesu anawayankha nati:

Yesu anayankha, Sanacimwa ameneyo, kapena atate wace ndi amace; koma kuti nchito za Mulungu zikaonetsedwe mwa iye. (Yohane 9:3)

MPHAMVU YA MULUNGU IMAKHALA PA IFE:

Ndipo ananena kwa ine, Cisomo canga cikukwanira; pakuti mphamvu yanga ithedwa m'ufoko. Cifukwa cace makamaka ndidzadzitamandira rriokondweratu m'maufoko anga, kuti mphamvu ya Kristu ikhale pa ine. (2 Akorinto 12:9)

ZINTHU ZONSE ZOSAKHAZIKIKA ZIMACHOTSEDWA PAMOYO WANU:

Zotsatira za chizunzo ndi zakuti zonse zimene ndi zosakhazikika zimachotsedwa pamoyo wanu. Mumasiya kudalira anthu, zinthu zakuthupi kapena zochitika zina ndi zina chifukwa zonsezi zimakhala kuti zakanika nthawi yansautso.

Mulungu akulonjeza kuti:

amene mau ace anagwedeza dziko pamenepo; koma tsopano adalonjeza, ndi kuti, Kamodzinso ndidzagwedeza, si dziko lokha, komanso m'mwamba. Ndipo ici, cakuti kamodzinso, cilozera kusuntha kwace kwa zinthu zogwedezeka, monga kwa zinthu zolengedwa, kuti zinthu zosagwedezeka zikhale. (Ahebri 12:26-27)

Munthawi ya mafunde amoyo, chinachilichonse chimene maziko ake si Mulungu simagwa. (Salimo 119:89 ndi Mateyu 7:24-27)

CHIDWI CHANU CHA ZOCHITA CHIMASINTHA:

Pamene mwakumana ndi nsautso, nthawi zambiri chidwi chanu chimagona pa chimene chayambitsa komanso zotsatira za nsautso kapena chizunzocho. Koma Mulungu akufuna kuti asinthe chidwi chathu kuti chichoke pa zithu zosakhalitisa ndi ndikukhazikika pa zinthu zamuyaya.

Pakuti cisautso cathu copepuka ca kanthawi citicitira ife kulemera koposa kwakukuru ndi kosatha kwa ulemerero; popeza sitipenyenera zinthu zooneka, koma zinthu zosaoneka; pakuti zinthu zooneka ziri za nthawi, koma zinthu zosaoneka ziri zosatha. (2 Akorinto 4:17-18)

Okonedwa, musazizwe ndi mayesedwe amoto adakugwerani inu akhale cakukuyesani, ngati cinthu cacilendo cacitika nanu: koma popeza mulawana ndi

Kristu zowawa zace, kondwerani; kutinso pa bvumbulutso la ulemerero wace mukakondwere kwakukurukuru. (1 Petro 4:12-13)

Ngati tipirira, tidzacitanso ufumu ndi iye: ngati timkana Iye, Iyeyunso adzaticana ife: (2 Timoteo 2:12)

CHIKHALIDWE CHATHU CHAKALE CHIMASINTHA:

Mulungu analankhula ndi mtundu wa moabu nati:

Moabu wakhala m'mtendere kuyambira ubwana wace, wakhala pansenga, osatetekulidwa, sananke kundende; cifukwa cace makoleredwe ace alimobe mwa iye, pfungo lace silinasinthika. (Yeremiya 48:11)

Chifukwa chakuti anthu aku moabu anali asanakumane ndi msautso kapena chiyesero cha chikhulupiriro chao, iwo sanali anthu osinthika. Iwo anakhala moyo otayilira ndipo anakhazikika pachuma chao. Sanakule muuzimu ngati mtundu wa anthu ndipo panalibe kusinthika kwina kulikonse pakati pao. Ndipo fungo lao lakale anali nalobe. Fungo la Moabu linali losasinthika.

Mazunzo amathandiza kuchotsa chikhalidwe chakale. Pamene mukutakasidwa, kukumana ndi mavuto a moyo, fungo lanu lachikunja limasinthika ndipo mumayamba kumveka fungo lauzimu.

MULUNGU AMAKHALA AKUKONZEKERETSANI UTUMIKI:

Ngati mukufuna kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu, kapena mufuna kufananizidwa ndi Yesu Khristu ndikukhala chotengeramo chake, Mulungu akhoza kuyankha zonsezi pogwiritsa ntchito chizunzo kapena nsautso.

Taona ndakuyenga, koma si monga siliva, ndakuyesa iwe m'ng'anjo ya masautso. (Yesaya 48:10)

Kudzera muchizunzo kapena nsautso, mumachoka pongakhala mwana wa Mulungu ndikukhala osankhidwa wake wa Mulungu. Mazuzo obwera chifukwa cha chifuniro cha Mulungu amakukonzekeeretsani kuti mukagwire ntchito moyenera.

MUMAKONZEKERETSEDWA KUTI MULAMULIRE NDI KHRISTU:

Ngati tipirira, tidzacitanso ufumu ndi iye: ngati timkana Iye, Iyeyunso adzaticana ife: (2 Timoteo 2:12)

MAZUNZO AMABWERETSA MADALITSO AUZIMU:

Yesu anati:

Odalaaliakuzunzidwacifukwa ca cilungamo: cifukwa uli wao Ufumu wa Kumwamba.

Odala muli inu m'mene adzanyazitsa inu, nadzazunza inu, nadzakunenerani monama zoipa ziri zonse cifukwa ca Ine. Sekerani, sangalalani: cifukwa mphotho yanu ndi yaikuru m'Mwamba: pakuti potero anazunza aneneri anakhalawo musanabadwe inu. (Mateyu 5:10-12)

MUMAPHUNZIRO KUMVERA KUDZERA MUMAZUNZO:

Angakhale anali Mwana, anaphunzira kumvera ndi izi adamva kuwawa nazo; (Ahebri 5:8)

MAU A MULUNGU AMAYESEDWA MKATI MWANU:

Mau a Yehova ndi mau oona; Ngati siliva woyenga m'ng'anjo yadothi, Yoiyeretsa kasanu ndi kawiri. (Masalmo 12:6)

MAZUNZO AMATITHANDIZA KUTI TIDZICHEPETSE:

Amene anakutsogolerani m'cipululu cacikuru ndi coopsaco, munali njoka zamoto, ndi zinkhanira, mouma mopanda madzi; amene anakuturutsirani madzi m'thantwe lansangalabwi; amene anakudyetsani m'cipululu ndi mana, amene makolo anu sanawadziwa; kuti akucepetseni, ndi kuti akuyeseni, kuti akucitireni cokoma potsiriza panu; (Deuteronomo 8:15-16)

MAZUNZO AMAPANGITSA KUTI MUKULE:

Pakufulua ine mundiyankhe, Mulungu wa cilungamo canga; Pondicepera mwandikulitsira malo: Ndcitireni cifundo, imvani pemphero langa. (Masalmo 4:1)

MUMAKHALA CHIFUPI NDI MULUNGU:

Mazunzo amathandiza kuti mukhale ndi ubale waukulu ndi Mulungu. Atakumana ndi nsautso waukulu, Yobu anazindikira choonadi chimenechi. Ndipo anati:

Kumva ndidamva mbiri yanu, Koma tsopano ndikupenyani maso; Cifukwa cace ndekha ndidzinyansa, ndi kulapa M'pfumbi ndi mapulusa. (Yobu 42:5-6)

Ambiri mwa ife timamudziwa Mulungu mwapamwambamwamba. Pamene zinthu zikuyenda Mulungu samakhalanso ofunika pamoyo wathu. Koma zinthu zikayamba kuvuta ndi pamene Mulungu amakhala ofunikira pamoyo wathu. Yobu anamudziwa Mulungu mozama pamene anakumana ndi nsautso. Izi sizikutanthauza kuti iye samamamudziwa Mulungu ayi, koma kumidziwa kwake kunali kungokhala ndi chidziwitso chabe cha Mulungu. Koma iye atakumana ndi nsautso, anamudziwa Mulungu kudzera munyengo zimene anadutsamo.

Paulo nayenso akufotokoza mfundo yomweyi:

Kuti ndimzindikire iye, ndi mphamvu ya kuuka kwace, ndi ciyanjano ca zowawa zace, pofanizidwa ndi imfa yace; (Afilipi 3:10)

Mukhodza kudziwa Mulungu kudzera muchiyanjano cha chizunzo.

Munyengo yonse yansautso wake, Yobu amafunsa Mulungu mafunso. Iye amaona ngati kuti gwero lan nsautso wa wake linali Mulungu. sikutu ndi zolakwika kufunsa Mulungu mafunso. Mwachitsanzo, ngakhale kuti Yesu amadziwa kuti cholinga chake chobwelera pa dziko lapansi chinali kudzapulumutsa munthu kumachimo, koma utafika nsautso, iye anafula nati, Mulungu wanga Mulungu wanga, mwandisiranji? Mau amene analakhula litatha funso limeneli ndi amene ali ofunika kwambiri chifukwa iye anati “mzimu wanga ndiupereka mmanja mwanu”

Ngakhale kuti Yobu anali ndi mafunso, koma iye anati:

Iye adzakhalanso cipulumutso canga, Pakuti wonyoza Mulungu sadzafika pamaso pace. (Yobu 13:16)

Koma ndidziwa kuti Mombolo wanga ali ndi moyo, Nadzauka potsiriza papfumbi. Ndipo khungu langa litaonongeka, Pamenepo wopanda thupi langa, ndidzapenya Mulungu; (Yobu 19:25-26)

Mafunso onse atatha, Yobu anachoka pakhazikika pa “iye” ndikukhazikika pa “Inu.” Muyenera kupereka nsautso wanu komanso mafunso onse osayankidwa mmanja mwa Mulungu.

Khulupirira Yehova ndi mtima wako wonse, Osacirikizika pa luntha lako; (Miyambi 3:5)

Mulungu amaonetsera pang’ono cholinga cha nsautso wanu, koma ndi zotheka kuti simungathe kumvetsa chinachilochonse.

Kubisa kanthu ndi ulemerero wa Mulungu; (Miyambi 25:2)

Zinsinsi nza Yehova Mulungu wathu; koma zobvumbuluka nza ife ndi ana athu kosatha, kuti ticite mau onse a cilamulo ici. (Deuteronomo 29:29)

Pali zinthu zina zobisika zimene ndi za Mulungu yekha. Ndipo ngati Yobu, mwina simungathe kumvetsa cholinga cha nsautso wanu.

Yehova alongosola mayendedwe a mwamuna; Munthu tsono angazindikire bwanji njira yace? (Miyambi 20:24)

Pamapeto azonze Mulungu atalankhula ndi Yobu pogwiritsan tchito zitsanzo zachilengedwe zimene Yobu sanathe kufotokozer. Mfumdo imene Mulungu amatsindika ndi yakuti ngati yobu samveta zitsanzo zakuthupi zimene ndi zooneka ndi maso, iye sakanamvetsa zinthu zosaoneka ndi maso za dziko lauzimu. Yobu atakumana ndi Mulungu, zinali zopanda ntchito kuti mafunso

ake analibe mayakho. Nkhawa zonse zobwera chifukwa chakuganiza kwa umuthu zinamuthera. Mayankho amafunso ake anali chikhulupiriro.

Pamene mwamudziwa Mulungu mwakuya kudzera muchizunzo, mumadziona mmene muyenera kudzionera. Zotsatira zokumana ndi Mulungu maso ndi maso zomakhala zoposa mafuso onse ndi kukambirana kungachite.

Pamene Yobu anafika pamaso pa Mulungu, panalibe yankho lina lilironse limene anakanapereka. Iye apatsidwa choonadi china chokhudza chizunzo. Mafunso ake onse anakhala opana kathu pamaso pa Mulungu ndipo panalibeso kukaika kwina kulikonse kumene anakhala nako.

SIMULI NOKHA

Pamene mukuzuzika malingani ndi chifuniro cha Mulungu, mukuyenera kuzindikira kuti simuli nokha. Okhulupirira ena ambiri nawoso akukumana ndi nkondo zomwezo:

ameneyo mumkanize okhazikika m'cikhulupiriro, podziwa kuti zowawa zomwezo zirimkukwaniridwa pa abale anu ali m'dziko. (1 Petro 5:9)

Namondwe wa moyo ndi osathawika, monga mowe zinawonetsedwera mufanizo la nyumba ziwiri pa Mateyu 7:24-27. Namondwe amabwera kwa onse amene amanga miyoyo yawo pa Mau a Mulungu komaso paonse amene sanamange pa Mau a Mulungu. Maziko a moyo wa Munthu ndi amene azawonetsere zotsatira zanomondwe.

Kuzuzika kukuyenera kuyembekezedwa monga ngati mbali imodzi ya chifuniro cha Mulungu:

Ndipo onse akufuna kukhala opembedza m'moyo mwa Kristu Yesu, adzamva mazunzo. (2 Timoteo 3:12)

kuti kwapatsidwa kwa inu kwaufulu cifukwa ca Kristu, si kukhulupirira kwa iye kokha, komatunso kumva zowawa cifukwa ca iye, (Afilipi 1:29)

kuti Uthenga Wabwino wathu sunadza kwa inu m'mau mokha, komatunso mumphamvu, ndi mwa Mzimu Woyera, ndi m'kucuruka kwakukuru; monga mudziwa tinakhala onga otani mwa inu cifukwa ca inu. (1 Atesalonika 1:5)

Pakutinso, pamenetinali ndi inu tinakuuziranitu kuti tidzamva zisautso; monga kudacitika, monganso mudziwa. (1 Atesalonika 3:4)

Pamenepo adzakuperekani kunsautso, nadzakuphani; ndipo anthu a mitundu yonse adzadana nanu, cifukwa ca dzina langa. (Mateyu 24:9)

Koma zisanacitike izi, anthu adzakuthirani manja, nadzakuzunzani, nadzapereka inu ku masunagoge ndi ndende, nadzamuka nanu kwa mafumu ndi akazembe, cifukwa ca dzina langa. (Luka 21:12)

Kumbukilani mau amene Ine ndinanena kwa inu, Kapolo sali wamkuru ndi mbuye wace. Ngati anandilondalonda Ine, adzakulonda-londani inunso; ngati anasunga mau anga, adzasunga anunso. (Yohane 15:20)

Koma izi sizikutanthauza kuti muzipangitse nokha kuzuzika mkumakhulupirira kuti zimusanagalatsa Mulungu. Mulungu samasangalala anthu akamazuzika. Kuzipanga nokha kuti muzuzike ndi tchimo.

Anthu ambiri amachita izi poyesa kumusanagalatsa, kuchotsa mkwiyo wa Mulungu kapena pofuna kuzipanga kuti aziwoneka oyera kapenso kuti aziwoneka achipembedzo kwambiri pamaso pa anthu. Koma Mulungu amasangalala ndi Mwazi wa Yesu Kristu okha. Koma Mulungu mmalo mwake amatenga zowawa zachizuzuo pamene zikukhudza moyo wanu ndikuwombola kukhala zabwino.

Mbali imodzi yandondomeko imene mpingo woyamba inakhazikitsa yotsatira onse amene akhulupirira kunali kufuna kuwaphunzitsa okhulupirira kuti adzakumana ndi mazuzo. Izi zikusowa mipingo yambiri lero:

nalimbikitsa mitima ya akuphunzira, nadandauliraiwo kuti akhalebe m'cikhulupiriro, ndi kuti tiyenera kulowa m'ufumu wa Mulungu ndi zisautso zambiri. (Machitidwe 14:22)

Mbali imodzi yoitanidwa ndi Yesu kukhala otsatira Wake ndi kuzikana ndi kuzuzika:

Ndipo 6 iye amene satenga mtanda wace, natsata pambuyo panga, sayenera Ine. (Mateyu 10:38)

Pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ace, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wace, nanditsate Ine. (Mateyu 16: 24)

Ndipo anadziitanira khamulo la anthu pamodzi ndi ophunzira ace, nati kwa iwo, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikanize yekha, nanyamule mtanda wace, nanditsate Ine. (Marko 8:34)

Ndipo Yesu anamyang'ana, namkonda, nati kwa iye, Cinthu cimodzi cikusowa: pita, gulitsa zonse uli nazo, nuzipereke kwa anthu aumphawi, ndipo cuma udzakhala naco m'mwamba; ndipo ukadze kuno, unditsate Ine. (Marko 10:21)

Ndipo iye ananena kwa onse, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikanize yekha, nanyamule mtanda wace tsiku ndi tsiku, nanditsate Ine. (Luka 9:23)

ndipo anatumiza kapolo wace pa nthawi ya phwando kukanena kwa oitanidwawo, idzani, cifukwa zonse zakonzeka tsopano. (Luka 14:27)

Yesu anaitana ophunzira kumoyo ozikana, mazuzo, ndi mtanda chifukwa cha kuthekera kwa mphamvu yachiyanjano mmazuzo Ake.

Mphamvu ya chiukitso ndi mphamvu ya mazuzo Ake ziri ngati mphamvu yambali yosiyana ya magetsi imene imagwiritsidwa ntchito padziko.

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Kodi gwero la machimo onse ndi kuzuzika ndi ndani?

3. Kodi kuvutika kumabwera bwanji miyoyo yanthu? Lembani njira zisanau zomwe zakambidwa muchaputalachi.

4. Lembani mwachidule zolinga pamphamvu zomwe zimakwaniritsidwa mumoyo mwa okhulupirira kupyolera mu kuzuzika.

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Ndi mbali ziti zamoyo wanu zomwe mukukumana ndi chizuzuo?

2. Kodi kuzuzika uku kumalowa bwanji mmoyo mwanu?

- Ena okuzungulilani
- Kupyolera zochitika mmoyo
- Chifukwa cha tchimo la inu mwini
- Chifukwa cha utumiki wanu
- Machitachita asatana

3. Kodi mwakhala mukuchitapo chani pokhudzana ndi chizuzochi?

Kuti Mulungu awonetsere mphamvu Zake kupyolera mukuzuzika, mukuyenera kusamalitsa mmene mukuchitira mkatikati mwachizuzocho. Simukuyenera kung'ung'udza ndi kudandaula. Uku kunali kuyakha kwa Aisraeli pakuzuzika. Anamuukira Mose (Eksodo 15:24). Koma kung'ung'udza konse kumakhala kuukira Mulungu. Zinthu zonse zimakuchitirani ubwino kuti mukafanane Makhalidwe ndi Yesu. Pamene mukudandaula chifukwa cha chizuzo, mumakhala mukudandaula molimbana ndi ndondomekoyi. Onani Aroma 8:28-29.

Pamene mukukumana ndi chizuzo, musamalole chikhalidwe chowawa kuti chitenge mbali. Kuwawidwa ndi kuyakha molakwikwa kuchizuzo, kudandaula, ndikukhala ndimalingaliro ofuna kubwezera. Ngati mulole kuwawidwa, kumakuzuzani komaso kukudetsani (Ahebri 12:16), kumakuletsani kuti musamve kuchokera kwa Mulungu (Eksodo 6:9), kumakulengerani mzimu ofuna kubwezera (1 Samueli 30:6), kumabweretsa kukhumudwa, komaso kupanda chiyembekezo (Maliro 3:18-20). Ndipo kumabweretsa ndulu yowawa ku uzimu wanu (Machitidwe 8:32).

4. Kodi mukhoza kuyakha bwanji kunyengo zovuta zanu molingana ndi njira yam mau?

CHAPUTALA 18

MMENE MUNGAKUMANIRANE NDI MPHAMVU YA MULUNGU

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osawonera.
- Kufotokoza momwe mungakumanirane ndi mphamvu ya Mulungu mmoyo mwanu ndi mutumiki mwanu.
- Kuwonetsera cholinga cha mpingo momwe umagwirizanirana ndi mphamvu ya uzimu.
- Kufotokoza mmene mphamvu ya uzimu imakulira.
- Kukumana ndi mphamvu ya uzimu mmoyo mwanu ndi mu utumiki.

VESI YOTSOGOLERA:

Ndipo iwowo anatuluka, nallikiraponse, ndipo Ambuye anachita nao pamodzi, natsimikiza mau ndi zizindikilo zakutsatapo. (Marko 16:20)

MAU OYAMBA

Mwaphunzira ndondomeko zambiri zamphamvu mu phunziro lino. Mu chaputala chino, ndondomeko zimenezi zalembedwa mwachidule ndipo chitsogozo chomaliza chaperekedwa kuti inu mukathe kukadzadzidwa ndi mphamvu ya uzimu yomwe mwamphunzira kale.

KULANDIRA MPHAMVU YA UZIMU

Mphamvu ya uzimu sichinthu choti mumalandira chifukwa chakuthekera kwanu. Sichimabwera chifukwa chophunzira mau. Ngakhale ndikukhala ndi chidziwitso cha Baibulo pa ndondomeko za mphamvu sichitsimikizo choti mulandira mphamvu ya uzimu.

Mphamvu ya uzimu imayenda kuchokera kuchiyambi kwake. Yesu akufanizidwa ndi mphesa, inu ndi mbali za uzimu. Simungabereke mphamvu mwainu nokha. Ndi moyo umene umayenda kuchokera komwe moyo umachokera. Mungolora mphamvu Yake kuti iyende kupyolera mwainu.

Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zace: wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala cipatso cambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kucita kanthu. (Yohane 15:5)

Iyi ndi ndondomeko ya Baibulo momwe mungadzadzidwire ndi mphamvu:

1. KUSALA KUDYA NDI KUPEMPHERA:

Bwerani pamaso ma Mulungu ndikuzichepetsa nokha kupyolera mukusala kudy a ndi kupemphera. Mulungu walonjeza kutimva pamene tafika chifupi Naye munchitidwe umenewu:

ndipo anthu anga ochedwa dzina langa akadzicepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zao zoipa; pamenepo ndidzamvera m'Mwamba, ndi kukhulukira coipa cao, ndi kuciritsa dziko lao. (2 Mberi 7:14)

Musamangofuna mphamvu yokhayo basi. Kupyolera mu pemphero ndi kusala kudy a kumakukozekeretsani kuti mukhale njira imene mphamvu ya Mulungu ingadulitsire.

2. KULANDIRA MPHATSO YA MZIMU WOYERA:

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Machitidwe 1:8)

3. KUGWIRITSA NTCHITO CHIKHULUPIRIRO:

Ndi chikhulupiriro, mumavomera lonjezano Lake la mphamvu:

Taonani, ndakupatsani ulamuliro wakuponda pa njoka ndi zinkhanira, ndi pa mphamvu iri yonse ya mdaniyo; ndipo kulibe kanthu kadzakuipsani konse. (Luka 10:19)

Koma cikhulupiriro ndico cikhazikitso ca zinthu zoyembekezeka, ciyesero ca zinthu zosapenyeka. (Ahebri 11:1)

Vomera chipulumutso ndi chikhulupiriro ndi kulandilaniso mphamvu ya Mulungu ndi chikhulupiriro. Kodi zimakhala zophweka bwanji kuvomera chipulumutso ndi chikhulupiriro koma zovuta kumukhulupirira Mulungu kuwonetsa mphamvu Yake mozizwitsa. Monga ngati kuchiritsa ndikutulutsa ziwanda?

4. NGWIRITSANI NTCHITO NDONDOMEKO ZA MPHAMVU ZA M'BAIBULO:

Mwachikhulupiriro yambani kugwiritsa ntchito ndondomeko za mphamvu za m'Baibulo. Izi mkuphatikizapo:

- **Mphamvu ya Uthenga Wabwino:** choyambirira moyo wanu ukuyenera kusithika kaye kupyolera mu mphamvu ya Uthenga Wabwino. Kulapa ndi maziko a chowonadi cha mphamvu ya uzimu
- **Mphamvu ya Mzimu Woyera:** mumalandira mphamvu kutsatira pamene Mzimu Woyera akadza pa inu.
- **Mphamvu ya chikondi:** mphatso iriyonse ya uzimu, kuwonetseredwa kulikonse kwa mphamvu kumakhala kopanda mpindu popanda chikondi.
- **Kudzodzedwa ndi mphamvu:** ndikudzodza kumene kumaphwasula goli. Simungachite ndi mphamvu zanu.
- **Mphamvu, chikhulupiriro, ndi ntchito:** izi sizingasiyanitsidwe. Zikuyenera kugwira ntchito limodzi mmoyo ndi utumiki wanu.
- **Dzina la Yesu:** Mumakhala pansu pa ulamuliro Wake. Ndi mphamvu kupyolera mu dzina Lake.
- **Mphamvu ya pemphero:** pemphero ndi kusala kudya kumabweretsa mphamvu za Uzimu.
- **Mphamvu ya Mau:** Muziyakhula Mau Ake, osati ainu eni. Mau Ake sazabwerera chabe kwa Iye. Azakwaniritsa cholinga chimene awatumira.
- **Mphamvu ya ulamuliro:** Khalanibe pansu pa ulamuliro kuti munthe kugwiritsa ntchito ulamuliro.
- **Mphamvu ya kuuka:** Mukumane nayo lero mu munthupi lanu la umunthu.
- **Mphamvu ya kuzuzika:** Mulindimphamvu mavuto komaso pamwamba pa mavuto. Kuyesdwa kwakukulu kumabweretsaso mphamvu yayikulu. Sithani kuvutika kwanu kukhala mwayi oti mphamvu ya Mulungu iwonekere.

MPHAMVU MU GWIRIZANO

Mphamvu ya uzimu okhulupirira aliyense akuyenera kukumana nayo payekha koma sikuyenera kugwiritsidwa ntchito pambali pa nthupi la Kristu. Ndi cholinga cha Mulungu kuti mpingo ukumane ndi mphamvu ya Mulungu mogwirizana. Mpingo ukuyenera kukhala pomwe mphamvu Yake ingawonetseredwe.

Tsiku lina Yesu anapita kukachisi ku Yelusalemu ndipo anapeza atsogoleri akugulitsa ng'ombe, nkhosa, ndi khunda. Anthu amenewa amkapanga phindu lalikuli kuchokera kwa anthu amene amkawagula kuti apereke msembe nyamazo. Amkagwiritsa ntchito tchalitchi monga ngati malo amalonda.

Yesu anawakwapula ndipo anawathamangitsa anthu onse tchalitchi. Anataya ndalama ndipo anagubuduza magome a anthu ositha ndalama nati...

Kwalembedwa, Ndipo nyumba yanga idzakhala nyumba yakupemphera; koma inu mwaiyesa iyo phanga la acifwamba. (Luka 19:46)

Mwanjira zambiri lero mpingo wasanduka malo achisangalalo ndi malo amkumano. Asanduka malo onogogawa chakudya ndi achisangalalo.

Zochitika zinazi zikhoza kukhala ndi malo ake, koma sicholinga cha Mulungu pa mpingo. Mpingo wowona umakhala ndiu gawo lamapephero ndi kuphunzitsana Baibulo komabe ukhoza kumasephana ndi cholinga cha Mulungu ngati zofuna za munthu zisidziwa malire ake. Mpingo umene Yesu anayeretsa unakhala unali pakati pa malonda. Koma Yesu anafotokoza cholinga chenichecha cha mpingo mu faniziro pa Luka 14:16-24. Mu faniziro iri, mbuye wa nyumba anawauza antchito ake:

Ndipo kapoloyo pakubwera anauza mbuye wace zinthu izi. Pamenepo mwini nyumba anakwiya, nati kwa kapolo wace, Turuka msanga, pita kumakwalala ndi ku njira za mudzi, nubwere nao muno aumphawi ndi opunduka ndi akhungu ndi otsimphina. Ndipo mbuye ananena kwa kapoloyo, Turuka, nupite kumiseu ndi njira za kuminda, nuwaumirize anthu alowe, kuti nyumba yanga idzale. (Luka 14:21, 23)

Mpingo ukuyenera kudzada ndi anthu amene ali ndi zosowa za umunthu. Okhulupirira akuyenera kupita kumadera onse ndi kufalitsa Uthenga Wabwino. Mpingo ukuyenera kudzada ndi okhulupirira amene ali ndi mphamvu ya uzimu. Izi zimapangitsa kuti pamalopo pakhale gwirizano omwe Mulungu antha kuziwonetsera Yekha. Olumala azachiritsidwa, akhungu

adzawona, osamva azamva, ndipo mphamvu ya Uthenga Wabwino izasitha miyoyo ya anthu ambiri.

Kumbukirani munthu wolumala amene anakhala apa chipata chakachisi ku Yerusalemu (Machitidwe 3). Machitachita achipembedzo anali akuchitika mkati mwakachisi. Kunali mwambo wokongola, mapephero oziwonetsera, kuimba kwanthetemya kumkachitika, koma osazindikira zosowa zake osakwaniritsidwa, panja pa nkomo la kachisi panakhala munthu osauka olumala. Kenako, amuna awiri, okhulupirira Mulungu amene anadzadzidwa ndi mphamvu ya uzimu, amkadutsa pa njira yake. Petro anati kwa iye, “Tayang’ana ife. Ndilinacho nacho ndikupatsa.” Pompo pompo, mapazi ake analimbikitsidwa ndipo anachiritsidwa ndi mphamvu ya Mulungu. Zosowa za dziko likuyang’ana pa ife. Anthu ozuzika maso awo akuyang’ana pa mpingo wa Yesu Kristu. Tikuyenera kukhala ndi chinachake choti tipereke.

LAMULO LOGWIRITSA NTCHITO NDI KUCHULUKITSA

Pali ndondomeko ya m’Bibulo yotchedwa kuti “Lamulo logwiritsa ntchito ndi kuchulukitsa” imene imakhudza mphamvu yauzimu. Mphamvu yanu yauzimu imachuluka ngati mugwiritsa ntchito bwino ndondomeko imeneyi. Werengani fanizo limene anaphunzitsa Yesu Pa Luka 19:12-26. Kapolo amene anagwiritsa ntchito ndikuchulukitsa ndalama zomwe anapatsidwa analandiraso zambiri zowonjezera. Wina amene sanazigwiritse ntchito anazitaya. “ Lamulo logwiritsa ntchito ndikuchulukitsa” ndi lakuti : Gwiritsani ntchito zomwe mwapatsidwa, ndipo zizachulukitsidwa. Mukuyenera kuzigwiritsa ntchito kapena kuzitaya. Mulungu wakupatsani mphamvu ya Uzimu ndi cholinga choti mutumikire, osati mulamulire (Mateyu 20:25-280. Ngati mugwiritsa bwino ntchito mphamvu ya uzimu, kuyenda kwa mphamvu ya Mulungu kuzachuluka mwa inu. Muzawona ngakhale kuwonetsera kwa mphamvu ya Mulungu kopambana mmoyo mwanu ndi muutumiki. Ngati simuigwiritsa ntchito, izakutayikani.

Ndipo wina anadza, nanena, Mbuye, taonani, siyi ndalama yanu, ndaisunga m'kansaru; (Luka 19:20)

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Lembani mwachidule ndondomeko zomwe zaperekedwa mu phunziro lino pamene mungakumanirane ndi mphamvu ya Mulungu.

3. Kodi cholinga cha Mpingo ndi chani pogwirizana ndi mpamvu ya uzimu?

4. Kodi mphamvu ya uzimu imachuluka bwanji?

(Mayankho amayesowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Mphamvu ya Mulungu imawonetseredwa kupyolera mu zizindikiro, zodabwitsa, ndi zozizwa. Werengani mavesi awa:

Eksodo 15:11

Numeri 14:22

Deutonomo 6:22; 7:19; 11:3; 29:3; 34:11

Yoswa 3:5

Nehemiya 9:10

Masalimo 77:11,14; 78:11,43; 88:10,12; 89:5; 96:3; 105:27; 136:4

Yeremiya 32:20

Danieli 4:2-3

Yoweri 2:30

Marko 16:17

Yohane 2:11,23; 3:2; 6:2,26; 7:31; 9:16; 11:47; 12:37; 20:30

Machitidwe 2:22,43; 4:30; 5:12; 6:8; 8:6,13; 14:3; 15:12; 19:11

Aroma 15:19

1 AKorinto 12:10, 28, 29

Agalatiya 3:5

Ahebri 2:4

CHAPUTALA 19

KULEPHERA KWA MPHAMVU

ZOLINGA:

Pomaliza paphunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osawonera.
- Kulozera kuchoka Mmalemba chifukwa cholepherekera mphamvu.
- Kupereka umboni wa Mmalemba umene umatsimikiza ukulu wa Mulungu munyengo zimene munthu sangathe kupeza mayankho.

VESI YOTSOGOLERA:

Ndipo Iye, chifukwa chakusakhulupirira kwao, sanachita kumeneko zamphamvu zambiri. (Mateyu 13:58)

MAU OYAMBA

Mu dziko lakunthupi, munthu amadalira mphamvu zakunthupi kuti apite patsogolo. Mphamvu zakunthupi zikhoza kukhala zophweka monga ngati moto umene umaphikiridwa chakudya. Kupanda moto, kuphika chakudya kumaima kaye. Mphamvu zakunthupi ndizosokonekera ngati mmene alirinso magetsi amene amakonzedwa mu mizinda ndi malo opangira magetsiwo. Pamene malo opangira magetsiwa alephera, nazo mphamvu zambiri zimalepherenso. Mzinda onse umapezeka kuti uli mundima. Pamene pali kulephera kwa mphamvu mudziko la kunthupi, kupita patsogolo kumaima kaye.

Izinso ziri chimodzimodzi mu dziko lakuuzimu. Pamene pali kulephera kwa mphamvu, kupita patsogolo kwa uzimu kumaima kaye. Miyoyo simasithika kupyolera mu mphamvu ya Uthenga Wabwino. Odwala samachiritsidwa. Ziwanda sizimalutsidwaso.

Pali zifukwa zimene zimapangitsa kuti mphamvu ileephere ku dziko la kunthupi. Chikhoza kukhala chifukwa chophweka, monga moto umene ukuyaka, kapena chifukwa chosokonekera, monga chidutswa chachipangizo chamakina owonongeka. Pamene zifukwa zimenezi zakulephera zadziwika ndi kukozedwa, kuyenda kwa mphamvu kumayambilanso.

Palinso zifukwa zina zimene zimapangitsa kuti mphamvu irephere mu dziko la uzimu. Pamene izi zazindikiridwa ndikukonzedwa, kuyenda kwamphamvu ya uzimu kumayambiranso.

KODI DZINA LANU LIMADZIWIKA KU JAHENA?

Chitsanzo chimodzi chachikulu chakulephereka kwa mphamvu ya uzimu kunalembedwa mu Machitidwe 19:13-16. Werengani nkhani imeneyi ya ana a mkulu wa msembe amene anayesera kutulutsa ziwanda mwa munthu ndipo analephera. Mzimu unalira mofuwula...

Ndipo unayankha mzimu woipa, nuti kwa iwo, Yesu ndimzindikira, ndi Paulo ndimdziwa, koma inu ndinu ayani? (Machitidwe 19:15)

Kenako munthu, amene anali ndi mzimu woipa, anawadumpira anyamatawo, mkuwang'ambira zovala zawo, ndipo anawavulaza. Anathawa amalimaliseche ndiposo ovulala kuchoka chifukwa munthu waziwandayo. Chiwanda chimkadziwa dzina la Paulo. Chiwanda chimkadziwa dzina la Yesu. Koma maina a anyamatawa samkadziwika chifukwa amkasowa mphamvu ya uzimu yeni yeni miyoyo yawo.

Ngati mwakhululukidwa machimo anu, dzina lanu limadziwika kumwamba. Limalembedwa buku la Mwana wankhonsa la moyo limene likunenedwa mu Chibvumbulutso 21:27. Kodi dzina lanu limadziwika ku Jahena? Kodi muli ndi mphamvu ya Mulungu imene ikuyenda mmoyo mwanu imene mphamvu ya ziwanda imatha kuzindikira ulamuliro wanu mu dzina la Yesu?

Amuna amenewa anayesa kugwiritsa ntchito dzina la Yesu kutulutsa ziwanda, koma izi sizinatheke. Dzina la Yesu simatsenga. Mukuyenera kukhala ndi mphamvu kumbuyo kwake. Mukuyenera kuizindikira ndi kukhala nawo ulamuliro wa dzina limeneli.

Mu ola lazovuta muzagonjetsedwa ngati dzina lanu likudziwika ku Jahena. Anthu amenewa sanakatha kumugojetsa satana potengera zomwe amkachita Paulo ndipo inuso simungakwanitse. Pokhapokha ngati mphamvu ya Mulungu ikuwonetseredwa mmoyo mwanu nde muzatha kumugonjetsa satana. Ngati mulibe mphamvu kuti dzina lanu silimadziwika ku Jahena, muzasiyidwa mutavulazidwa ndiposo wamaliseche pamaso pa mdani.

KULEPHERA KWA MPHAMVU

Nazi zifukwa zina zimene zimapangitsa kuti mphamu ilephere:

TCHIMO:

Tchimo limalekanitsa munthu kwa Mulungu. Pamene mwalekanitsidwa ndi Mulungu, mphamvu Yake singayende mwainu.

Werengani Aroma 7 pamene mtumwi Paulo akunena zakulimbana kwake ndi goli la tchimo. Werengani kumasulidwa kwake mu Aroma 8. Monga ngati wokhulupirira, Paulo analiso ndi kulimbana ndi tchimo kumene inuso mwakumana nako, koma anaphunzira kupambana lamulo la tchimo limene limkagwira ntchito nthupi mwake. Chifukwa cha ichi, moyo wake unatsekuka kukuyenda kwa mphamvu ya Mulungu.

Pamene munthu wochimwa dzina lake Simoni anapereka ndalama kuti agule mphamvu ya uzimu, Petro anayakha:

Ulibe gawo kapena colandira ndi mau awa; pakuti mtima wako suli wolunjika pamaso pa Mulungu. Cifukwa: cace lapa coipa calm ici, pemphera Ambuye, kuti kapena akukhulukire iwe colingiriraca mtima wako. Pakuti ndiona kuti wagwidwa ndi ndulu yowawa ndi nsinga ya cosalungama. (Machitidwe 8:21-23)

Kulapa machimo ndikukhulukidwa kupyolera mu mwazi wa Yesu Kristu ndi njira yokhayo yolumikiza kusiyanaku. Tchimo limatirekanitsa ndi mphamvu ya Mulungu. Pamene Yesu azabweraso...

Atesalonika 1:8 m'lawi lamoto, ndi kubwezera cilango kwa iwo osamdziwa Mulungu, ndi iwo osamvera Uthenga Wabwino wa Ambuye wathu Yesu; (2 Atesalonika 1:8)

Onse amene ali mu tchimo aza...

amene adzamva cilango, ndico cionongeko cosatha cowasiyanitsa ku nkhope ya Ambuye, ndi ku ulemerero wa mphamvu yace, (2 Atesalonika 1:9)

Pamapeto ake, tchimo lizabweretsa kusiyanitsidwa kwamuyaya ndi mphamvu ya Mulungu.

UKAPOLO:

Ukapolo wauzimu umatha ku tchinga kuyenda kwa mphamvu ya Mulungu mmoyo mwanu. Ukapolo si tchimo paokha. Ndi zinthu kapena zochitika zimene zimasanduka kukhala zofunika kwambiri kwa inu zomwe mmakhala pansi paulamuliro wake. Paulo analemba:

Zinthu zonse ziloledwa kwa ine; koma si zonse zipindula, Zinthu zonse ziloledwa kwa ine, koma sindidzalamulidwa naco cimodzi. (1 Akorinto 6:12)

Chirichonse mmoyo mwanu chimene chikudya maganizo ndizofuna zanu chimenecho ndi ukapolo. Mamakhala pansi pa mphamvu yake.

Zikhoza kukhala zokonda kapena chizolowezi. Akhoza kukhala malingaliro oipa ndi matha amene amakutchingani kuti musachite mwachikhulupiriro ndi mphamvu. ukapolo oterewo amapangitsa kuti mphamvu irephere chifukwa mmakhala pansi pa mphamvu pawo malo mwa mphamvu ya Mzimu Woyera.

KUSOKONEZA NDONDOMEKO ZA MPHAMVU:

Mwaphunzira ndondomeko zamphamvu za m'Baibulo zochuluka mu phunziro lino. Kusokoneza ndondomeko zimenezi zotsatira zake ndikulephera kwa mphamvu.

KULAMULIRA MMALO MOTUMIKIRA:

Pamene mphamvu ya uzimu ikugwiritsidwa ntchito kulamulira mmalo otumikira, kulephera kwa mphamvu kumachitika. Munaphunzira mu Mateyu 20:25-28 kuti ndondomeko ya mphamvu ya Mulungu siri monga mmene iriri yapadziko pano. Malingaliro amphamvu yapadziko ndiko kulamulira ena.

Kuchokera ku umwana, timakhala tikufunafuna mphamvu ya padziko. Timakhala tikuwalamulira ndi kuwapusitsa makolo athu. Timakhala tikufuna mphamvu mdera lathu, pa zomwe zatizungulira, ngakhalenso timayesa kulosera ndi kulamulira mphamvu ya chilengedwe.

Ndondomeko ya mphamvu za Baibulo imaitani kotumikira ndi kukumana ndi zosowa za anthu kupyolera kuwonetsera kwa mphamvu ya Mulungu. Paulo anawalemba okhulupiria aku Akorinto pa mutu umenewu. Monga ngati mtumwi wamkulu wa mpingo, Paulo anali ndi ulamuliro pa gulu limeneri la okhulupirirawa. Koma sanagwiritse udyo mphamvu imeneyi.

Anawauza iwo:

Ngati ena ali nao ulamuliro umene pa inu, si ife nanga koposa? Koma sitinacita nao ulamuliro umene; koma timalola zonse, kuti tingacite cocedwetsa kwa Uthenga Wabwino wa Kristu, (1 Akorinto 9:12)

Paulo sanagwiritse ntchito udyo udindo wake wa uzimu. Sanawalamulire Akorinto, mmalo mwake anawatumikira iwo:

si cifukwa tiribe ulamuliro, komatu kuti tidzipereke tokha tikhale kwa inu citsanzo canu, kuti mukatitsanze ife. (2 Atesalonika 3:9)

KUPEZA PHINDU INU ENI:

Paulo anawalemberaso Akorinto zokhudzana mphamvu zopindulira iye mwini. Anati:

Ngati takufeserani inu zauzimu, kodi ncacikuru ngati ife tituta za thupi lanu? (1 Akorinto 9:11)

Paulo anagwira ntchito pakati pa Akorinto ndipo anafesa mbeu ya uzimu. Anali ndi ufulu wolandira kuchokera kwa iwo”zinthu zakuthupi” makamaka thandizo lazachuma. Koma sanagwiritse udyo mphamvu imeneyi. Anasakha kuvutika kusiyana kugwiritsa udyo mphamvu yauzimu ndi kutchinga ntchito ya Mulungu (1 Akorinto 9:12)

Yesu anayesedwa ndi satana kuti agwiritse ntchito mphamvu yake popindula iye mwini. Satana anamuyesa Iye kuti asandutse mwala kukhala mkate ndi kuwonetsa mphamvu Yake kwa anthu podumphama pamwamba pa kachisi. Yesu anakana.

Pamene Yesu amkazuzika pamtanda chifukwa cha machimo a anthu onse, anakatha kuitana angelo 10,000 kuti abwere kuzamupulumutsa (Mateyu 26:53). Anakana kuwonetsera mphamvu kotereko kuti akakwaniritse cholinga chachikulu cha Mulungu.

KUKOPERA:

Mwaphunzira mbuyomu mu phunziro la tchimo la thupi lotchedwa “kukopera” lomwe ndi kaduka komwe kamawonetsedwera pokopera ena (Agalatiya 5:20). Iri linali vuto lomwe linabweretsa kulephera kwa mphamvu mu mpingo woyamba. Machitidwew 19:13 akuyakhula za onse amene anatengera “pa iwo okha” poyesa kutulutsa ziwanda pokopera utumiki wa Paulo.

Pamene mukuyesera kukopera mautumiki a ena, makumana ndi kulephera kwa mphamvu koopsy munga mmene anthu awa anachitira.

ZOLINGA ZOLAKWIKWA:

Musamasilire chifikwa mphamvu za uzimu nthawi zina zimagwiritsidwa ntchito molakwika. Mphamvu ya Uzimu imene imayenda kuchokera kwa Mulungu ndi yabwino, koma ikhoza kugwiritsidwa ntchito udyo ndipo ndi cholinga cholakwika ndi maganizonso olakwika.

Tchimo loyamba la satana linabwera chifukwa cha maganizo olakwika ofunafuna mphamvu. Izi zirinso chimodzi modzi ndi tchimo loyamba la munthu lomwe linachitidwa posakasaka mphamvu yomwe imabwera ndi chidziwitso.

Yakobo ndi Yohane nthawi ina amkafuna aitanitse moto kuchokera kumwamba kuti awotche anthu onse amene amatsutsana ndi Yesu. Kunakakhala kuwonetsera mphamvu kozizwa kotani uku! Koma cholinga chao chinali cholakwika. Cholinga chao kunali kufuna kubwezera pa adani onse, kuwonetsera kotere kunakakhala kugwiritsa ntchito udyo mphamvu ya uzimu. Yesu anawauzo iwo:

Koma iye anapotoloka nawadzudzula. Ndipo anapita kumudzi kwina. (Luka 9:55-56)

Zolinga zosayenera zimabweretsa malingaliro olakwika okhazikika pa mphamvu. Yesu anachenjeza ophunzira Ake:

Taonani, ndakupatsani ulamuliro wakuponda pa njoka ndi zinkhanira, ndi pa mphamvu iri yonse ya mdaniyo; ndipo kulibe kanthu kadhakwipsani konse. Koma musakondwera nako kuti mizimu idakugonjerani, koma kondwerani kuti maina anu alembedwa m'Mwamba. (Luka 10:19-20)

KUSAKHULUPIRIRA:

Chifukwa chachikulu chimene chimapangitsa kuti mphamvu ya uzimu irephere ndi kusakhulupirira. Kusakhulupirira ngakhaleso kunakhudza utumiki wa Yesu:

Ndipo Iye, cifukwa ca kusakhulupirira kwao, sanacita kumeneko zamphamvu zambiri. (Mateyu 13:58)

Kuwonetsera mphamvu ya Mulungu kukhoza kusokonezedwa ndi kusakhulupira kwa onse amene mukuwatumikira. kusakhulupira kwa inu eni Kukhozaso kusokonezanso (Mateyu 17:14-21)

KUMPATSA MALIRE MULUNGU:

Mphamvu ya Mulungu ilibe malire, koma tikhoza kuika malire momwe ingagwirire ntchito mwa ife. Paulo ananena kuti Mulungu ndi wothekera kuchita mopitirira monga ife tipephera kapena kuganiza malingana ndi mphamvu imene imagwira ntchito mwa ife.

Ndipo kwa iye amene angathe kucita koposa-posatu zonse zimene tizipempha, kapena tiziganiza, monga mwa mphamvu ya kucita mwa ife, (Aefeso 3:20)

Nthawi zina Mulungu samachita malingana ndi mmene ife tikufunira kapena kuganizira chifukwa sitirola mphamvu Yake kuti igwire ntchito mwa ife.

PAMENE PALIBE ZOZIZWA

Pamene okhulupirira akukumana ndi kulephereka kwa mphamvu ya uzimu, zonse zimene takambirana zikuyenera kuunikidwa ndi pemphero. Pamene chisokonezo chimenechi chazindikiridwa, zikuyenera kukozedwa ndi cholinga chakuti mphamvu ya Mulungu iyambireso kuyenda popanda chotchinga.

Kodi nanga zitakhala kuti zonsezi zakozedwa, koma zozizwa sizikuchitibe? Cholinga chingakhale chani kuti munthu wina wamasulidwa pakuyakhidwa kwa mapephero athu pamene wina ayi? Nazo zitsanzo zeni zeni za moyo:

- Banja lina la chikhristu linali ndi ana awiri ang'ono. Onse anadwalika kwambiri. Onse anapephereredwa ndi makolo awo onse ndi gulu limodzi la akhristu okhulupirira. Mmodzi anachiritsidwa ndipo ndi mtumiki wa Uthenga Wabwino lero. Pamene winayo sanachiritsidwe. Anakhala zaka zambiri akudwala ndipo mapeto ake anamwalira.
- Mtumiki wina wodziwika bwino wakunja amene Mulungu amamugwiritsa ntchito mwamphamvu pochiritsa tsiku lina ananena kuti anthu okwana 10% amene anawapepherera anachiritsidwa.

- Petro yemwe amene anapephereredwa ndi okhulupirira mkutuluka ku ndende patsogolo anaphedwa chifukwa cha Uthenga Wabwino. Nchifukwa chani mphamvu yomwe ija inatsekula zitseko za ndende sinamupulumutse ku imfa yowawayi?
- Kunali akhate ambiri ku Israeli mu nthawi ya Eliya, koma mmodzi yekha anachiritsidwa ndi Mulungu (Luka 4:27).

Tiribe mayankho amafunso amenewa. Ngati tingakhale ndi mayankho ndi chidziwitso chonse, nde kuti tinakakhala ngati Mulungu. Tikuyenera kuzindikira ukulu wa Mulungu mu madera amphamvu ya uzimu. Timagwira ntchito ndi mphamvu yopatsaidwa. Ndi mphamvu ndiye kuti iri panso pa ulamuliro wawina.

Pa mafunso amene sitingathe kupezera mayankho ake, Baibulo limanena kuti...

Zinsinsi nza Yehova Mulungu wathu; koma zobvumbuluka nza ife ndi ana athu kosatha, kuti ticite mau onse a cilamulo ici. (Deutoronomo 29:29)

Munyengo zina, Mulungu amawonetsera chifukwa chimene zozizwa sizikuchitikira. Mu nthawi zina, sitingathe kupeza mayankho. Kuli zinthu zina zobisika zodziwika ndi Mulungu yekha. Timagwira ntchito mulingo wa chibvumbulutso, osati ndi kuzindikira kwa muyaya. Koma musalole izi kuti zitchinge kuwonetseredwa kwa mphamvu ya Mulungu pa moyo wanu. Muziyenda muzimene zabvumbulutsidwa. Mafunso osayakhidwa asiyeni chifukwa zina ndi zinsisi za Mulungu.

Mphamvu ya Mulungu imawonekera mu imfa ndi mmoyo momwe. Imawonekera muzodziwika ndi zosamvetsetseka ngakhaleso muzonse zimene sizikudziwika. Imawonetseredwa mu chifooko ngakhaleso mu mphamvu.

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Perekani umboni wamalemba umene umatsimikiza umuyaya wa Mulungu mu zochitika zimene munthu sangathe kupeza mayankho.

3. Lembani mwachidule zimene mwaphunzira mu chaputala chimo zokhudzana ndikulephera kwa mphamvu ya uzimu.

(Mayankho amayesowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Werengani nkhani ya Davide ndi Batisheba mu 2 Samueli chaputala 11. Davide anagwiritsa ntchito udyo mphamvu zake zopatsidwa ndi Mulungu monga mfumu ndipo anachita tchimo lachigololo, kutenga mkazi wa munthu wina, ndiposo ndikupha mamuna wake. Onani momwe mneneri wa Mulungu anatsindikira kusagwiritsa bwino ntchito mphamvu podzudzula mu 2 Samueli 12:1-14.
2. Mneneri wa Chipangano Chakale dzina lake Balamu nayeso anagwiritsa udyo ntchito mphamvu ya Uzimu yopatsidwa ndi Mulungu kwa iye. Werengani nkhani yake mu Numeri 22-24.
3. Machitidwe 8:9-11 ikukamba za ubwino wozindikira mphamvu ya Mulungu yeniyeni kuti pakutero musanyengedwe ndi onse amene amagwiritsa ntchito udyo mphamvu ya uzimu.
4. Werengani nkhani ya Yoasi mu 2 Mafumu 13:18-19. Ambuye ndi mneneri anakhumudwa chifukwa cha Yoasi sanagwiritse ntchito mphamvu zonze zimene Mulungu anamupatsa. Analandira kuchokera kwa Mulungu, pazomwe anakhulupira zokha. Sanalandire zonse zimene Mulungu amafuna kuti ampatse iye chifukwa anaika malire aumunthu wake.

CHAPUTALA 20

KUKUMANA NDI ZOTCHINGA

ZOLINGA:

Pomaliza za phunziroli mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osawonera.
- Kuloza gwero limene lirikumbuyo kwa zotsutsana ndi mphamvu ya uzimu ndi ulamuliro.
- Kufotokoza zifukwa zimene ulamuliro wa uzimu umakuma ndi zotsutsa.
- Kulemba ndondomeko zokumanirana ndi zotchinga.

VESI YOTSOGOLERA:

Adzikhazikitsa mafumu adziko lapansi, nachita upo akulu pamodzi, kutsutsana naye Yehova, ndi Wodzodzedwa wake...(Masalimo 2:2)

MAU OYAMBA

Mphamvu ndi ulamuliro wa Yesu inatsutsidwa kawirikawiri pa nthawi ya utumiki wake padziko lapansi. Pamene Yesu anabatizidwa mmadzi ndipo mphamvu ya Mzimu Woyera inadza pa Iye, mphamvu Yake inayesedwa ndi satana mukuyedwe komwe kunachitika magawo atatu (Mateyu 4:1-11).

Satana anamuyesa Yesu kuti agwiritse mphamvu Zake pomupindulira Iye mwini posandutsa mwala kukhala mkate. Anamuyesaso Yesu kuti awonetse mphamvu Yake podumpha kuchokera padenga la kachisi. Satana anapereka mafumu onse a padziko lapansi pokhapokha ngati Yesu angamulambire iye.

Ulamuliro wa Yesu unatsutsidwaso ndi atsogoleri achipembedzo anthawi imeneyo. Anatsutsana ndi chiphunzitso chake, mmene amakhalira, ndi mmene anawotsera mphamvu ya Mulungu mmoyo Mwake ndi utumiki omwe.

KUSERI KWA CHOTSUTSA

Mu chaputala 3 cha phunziro lino mwaphunzira zokhudzana “Kulimbana ndi chinyengo.” Nthawi zonse kumbukirani kuti satana ndi amene ali kuseli kwa chotsutsa cha mphamvu ya uzimu yeniyeni.

Zotsutsa zina za mphamvu ya uzimu zimabwera chifukwa chazochitika za moyo. Zovuta zadziko zikhoza kukhala zazikulu ndi zambiri. Satana amakhala kumbuyo kwazochitika zimene zimatchinga kuyenda kwa mphamvu ya Mulungu mmoyo mwanu.

Zotsutsa zina zimabwera kupyolera mwa anthu amene akuzungulirani, koma nthawi zonse muzikumbukira kuti si anthuwo paokha amene akutsutana nanu. Amalora maganizo awo ndi makhalidwe awo kuti zilamuliridwe ndi satana. satana ndi amene ali kumbuyo kwamphamvu imene imalimbana ndi mphamvu yanu yauzimu ndi ulamuliro.

ZIFUKWA ZA CHITSUTSO

Panali zifukwa zomwe zinapangitsa kuti ulamuliro wa Yesu utsutsidwe. Ndi zifukwa zomwezo zimene zizapangitse satana kuti atsutsaneso ndi mphamvu yanu ya uzimu.

KUSAKHULUPIRIRA:

Werengani nkhani ya kudzutsidwa kwa mwana wa mkazi wa Yayero kuchokera kwa akufa pa Luka 8:49-56. Yesu anachita zozizwa zazikulu, koma asanachite anakumanaso ndi vuto lofanana ndi zotsutsa zimene inu mutakumane nazoso.

Pamene Yesu analowa mnyumba ya Yayero anakumana mkusakhulupirira. Pamene mukukhulupirira kuwonetseredwa kwa mphamvu Yake, anthu opanda chikhulupiriro azakuuzani chifukwa chomwe sizingathekere, ndi chifukwa chiyani sichiri chifuniro cha Mulungu kuti izi zichitike.

MALINGALIRO OTCHUKA:

Musaganize molakwitsa dala poganiza kuti chifukwa muli ndi mphamvu ya Mulungu ndekuti muzakonedwa ndi wina aliyense. Maganizo otchuka anatsutsana ndi mphamvu ya Yesu. Werengani nkhani imene iri pa Marko 5:5-15. Yesu anachita chozizwa chachikulu, koma maganizo otchuka analimbana naye.

Ndipo anayamba kumpempha Iye kuti acoke m'malire ao, (Marko 5:17)

Pa nthawi ina, anthu anamuseka Yesu (Marko 5:40). Mukuyenera kukhala okonzeka, ngati mungathe, kuima panokha. Siwina aliyense azalandira utumiki wanu. Kunanenedwa kuti masiku amaliza anthu azaziunjikira okha aphunzitsi “okhala ndi makutu oyabwa.” Mautumiki otchuka

azakhala amene azanene zimene anthu azafune kumva mmalo mwa uthenga umene Mulungu akufuna kuti apereke.

CHIKHALIDWE:

Alembi ndi Afalisi anatsutsana ndi ulamuliro wa Yesu chifukwa sumkagwirizana ndi chikhalidwe chachipembedzo chao. Yesu kawirikawiri amkati “munamva”ndipo amkanena za chikhalidwe za chipembedzo cha atsogoleriwo. Kenako amkanena kuti “Koma ndindena ndi inu,”ndipo amkapitiriza kugawa chowonadi chenicheni chochokera kwa Mulungu. Yesu anakumana ndi chitsutso chifukwa chiphunzitsa Chake cha mphamvu ndi ulamuliro sumkagwirizana ndi chikhalidwe chochita kupangidwa ndi munthu.

Kuwonetsera kwa mphamvu ya Mulungu sikungavomerezedwe ndi chikhalidwe cha mtundu wanu kapenaso chipembedzo chanu. Ngati izi zirizowona, nde kuti muzakuma ndi chotsutsa pa chifukwa chomwecho Yesu anatsutsidwa.

NYOTA:

Ulamuliro wa Yesu unatsutsidwa chifukwa sanavomerezedwe ndi atsogoleri achipembedzo. Sanali ndi nyota ina iriyonse ya Alembi kapena Chifalisi. Atsutsana ndi ulamuliro Wake chifukwa anali mwana wa mpala matabwa wochokera kumudzi osauka wa Nazareti:

Kodi uyu si mwana wa mmisiri wa mitengo? kodi dzina lace la amace si Mariya? ndi 5 abale ace si Yakobo ndi Yosefe ndi Simoni ndi Yuda? Ndipo alongo ace sali ndife onsewa? Ndipo iyeyo adazitenga zinthu zonsezi kuti? (Mateyu 13:55-56)

Ngakhalenso wina amene amayembekezera kuti azakhale Ophunzira Wake anafusa:

Natanayeli anati kwa iye, 13 Ku Nazarete nkutha kucokera kanthu kabwino kodi? Filipino ananena naye, Tiye ukaone. (Yohane 1:46)

Anthu anafunsa:

Ndipo m'mene Iye analowa m'Kacisi, ansembe akuru ndi akuru anthu anadza kwa Iye analikuphunzitsa, nanena, Mucita izi ndi ulamuliro wotani? Ndipo ndani anakupatsani ulamuliro wotere? (Mateyu 21:23)

Mphamvu ndi ulamuliro wanu uzatsutsidwa ndi anthu amene amayesa kuti inu simuchokera ku mtundu woyenera, kapena kupeza kwanu mkwapasi. Muzatsutsidwaso chifukwa simunapite ku sukulu ya Baibulo kapenaso mulibe nyota ya mpingo uliwonse.

Ndi kofunika kwambiri kukhala ndi nyota ya mphamvu ya uzimu kusiyana ndi ya chipembedzo chamunthu. Chofunikwa kwambiri ndi kukhala mamuna kapena mkazi amene wamvomeredzwa ndi Mulungu (Machitidwe 2:22).

CHIPHUNZITSO:

Yesu anatsutsidwa chifukwa chachiphunzitso Chake:

Ndipo anazizwa onse, kotero kuti anafunsana mwa iwo okha, kuti, Ici nciani? ciphunzitso catsopano! ndi mphamvu alamula ingakhale mizimu yonyansa, ndipo imvera Iye. (Marko 1:27)

Mphamvu imene inawonetsedwa ndi Yesu sinafanane ndi ziphunzitso zomwe atsogoleri azipembedzo anali nazo mu nthawi imeneyo. Ziphunzitso Zake sizimkagwirizana ndi mfundo ndi zikhulupiriro zimene zinaikidwa mkumatchulidwa kuti ziphunzitso.

KHALIDWE LOPHUNZITSIRA:

Ena anatsutsa ndi mchitidwe umene Yesu amkaphunzitsira. Anaphunzitsa ndi ulamuliro, asati ndi kuzimiririka kumene amkagwiritsa ntchito Alembi. Ena azakutsutsani ndi momwe muperekerwa chiphunzitso. Azanena kuti muli ndimachitachita ambiri kapenaso mukuphunzitsa ndi ulamuliro wochulukira.

Kupereka kwa chiphunzitso kwa Yesu kunali kophweka, koma kwamphamvu. Ena azakulangizani kuti muziralikira mwaphamvu, uthenga wa chiphunzitso cha Mulungu okhala ndi zitsanzo ndi machitachita ochepa. Koma kumbukira zomwe Paulo ananena:

Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'cionetso ca Mzimu ndi ca mphamvu; kuti cikhulupiriro canu cisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu. (1 Akorinto 2:4-5)

KULAKWITSA KWA UZIMU:

Kuwonetsera kwa mphamvu ya Mulungu kumatsutsidwa:

Koma Yesu anayankha, nati kwa iwo, Mungolakwa osadziwa malembo, kapena mphamvu za Mulungu. (Mateyu 22:29)

Mukhoza kutsutsidwa ndi onse amene akukhala mukulakwitsa kwa uzimu chifukwa amakana mphamvu ya Mulungu.

KUGWIRITSA NTCHITO BWINO:

Muzatsutsidwa ndi anthu amene azakuyeseni kuti mugwiritse ntchito molakwikwa mphamvu ya uzimu. Yesu anatsutsidwa ndi satana mu dera limeneri. Anamuyesa Yesu kuti agwiritse ntchito mphamvu Zake pazopindulitsa Iye mwini kuti akawonetsere mphamvu Yake.

Satana azakuyesani chimodzimodzi mwa mtundu umenewu. Azakuyesani kuti mugwiritse ntchito molakwika ulamuliro kuti mupeze malo aulemerelo. Azakupatsani maganizo anjira zimene mungagwiritsire mphamvu pofuna kuti inu mwini mupindule. Chimenechi ndi chotsutsa chachikulu chimene muzakumane nacho.

KUYENDA KWA MOYO WANU:

Muzakumana ndi chitsutso pamene mukukhala moyo wachikhulupiriro ndi mphamvu. Onse amene akuyenda ndi chikhulupiriro anakhala choyambwa kwa onse amene akuyenda ndi zowoneka ndi maso.

Sitifano anali munthu wachikhulupiriro ndi mphamvu (Machitidwe 6:8). Makhalidwe a moyo wake ndi umboni u woyabwa kwa atsogoleri achipembedzo anthawi imeneyo amene anapwetekedwa mtima (Machitidwe 7:54) ndipo anamugenda iye ndi miyala mpakana kumwalira.

KUKUMANA NDI CHOTSUTSA

Pamene mukuyenda kupitirira mulingo wa madalitso a uzimu kufika ku mulingo wa mphamvu ndi ulamuliro, nanunso muzakumana ndi zokutsutsani. Izi ndi zoyenera kuchita pamene satana atsutsana ndi ulamuliro wanu:

KUZINDIKIRA KOCHOKERA:

Kumbukirani kuti zotsutsana ndi mphamvu ya uzimu zimachokera kwa satana. sizochitika kapene anthu amene ali zotsutsa. Mukuyenera kuzindikira kochokera kwenikweni kwa zokutsutsani kuti muthane nazo bwino:

Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:12)

MUSAMATAYE NTHAWI PAMTSUTSO:

Chifukwa chakuti nkondo yanu siri yanthupi ndi mwazi, musamataye thawi pomatsutsana ndi munthu. Satana samasokonekera ndi kuganiza, nzeru, kapena mtsutso zokhudzana ndi zophunzira zokhudzana Mulungu.

Yesu sanataye nthawi Yake pochita mtsutso wokhudzana ndi ulamuliro Wake wauzimu. Anafunsa mafunso ochepa omwe ankalanjika pamakhalidwe auzimu a omwe amkatsutsana Naye, ndipo kenako anati...

Ndipo anamyankha Yesu, nati, Sitidziwa ife. Iyenso ananena nao, Inenso sindikuuzani ndi ulamuliro wotani ndizicita izi. (Mateyu 21:27)

KUKUMANA NDI CHITSUTSO:

Musamathawe kukumana ndi chitsutso. Musamaimitse kuyenda kwa mphamvu ya Mulungu ndi cholinga choti musangalatse anthu. Mukumane ndi chitsutso mu mphamvu Mulungu.

Pamene Yesu analowa m'nyumba ya Yayiro kukamudzutsa mwana wake wa mkazi anakumana ndi mphamvu yakusakhulupirira. Sanalolere kuti izi zimuletse. Sanatuluke mnyumbambo mothawa kapena kugonjetsedwa. Anakumana ndi chitsutso ndipo anakwaniritsa cholinga Chake chimene anabwerera.

TENGANI ULAMULIRO:

Kumbukirani ulamuliro umene unapatsidwa kwa inu ndi Yesu. Anati “Ndakupatsani mphamvu zonse pa mphamvu za mdani.”

Wapereka mphamvu zimenezi kwa inu, koma mukuyenera kuzigwiritsa ntchito. Pamene mukukumana ndi chitsutso cha satana, tengani ulamuliro wa uzimu pa chotsutsacho. Tengani ulamuliro mu dzina la Yesu. Tengani ulamuliro malingani ndi mmene Mau a Mulungu akunenera. Gwiritsani ntchito Ndi ndondomeko za mphamvu zomwe mwaphunzira mu phunziro lino.

Mwapatsidwa mphamvu pamwamba pa mphamvu zonse za mdani. Popambana mphamvu zonse zosakhala bwino zosakhulupirira! Tengani malo anu oyenerera a ulamuliro mwa Mulungu.

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Kodi ndi ndani amene alikumbuyo kwa komwe kumachokera zotsutsana ndi mphamvu ya uzimu yeniyeni?

3. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira mu phunziro lino zokhudzana ndi zifukwa zomwe mphamvu ndi ulamuliro umatsutsidwa.

4. Lembani njira zomwe zaperekedwa mu chaputala chino zokumanirani ndi zotchinga za mphamvu ya uzimu.

(Mayenso amayesowa aperekedwa kumapeto abukuli)

MAYANKHO AMAYESO OZIYENSA NOKHA

CHAPUTALA 1:

1. Inu Mulungu, ndinu Mulungu wanga; ndizakufunani m' matanda kucha: Moyo wanga ukumva ludzu la kwa Inu, thupi langa lilirira Inu, Mdziko louma ndi lotopetsa, lopanda madzi. Kuti ndione mphamvu yanu ndi ulemerero wanu, monga ndinakuonani m' malo oyera. (Masalimo 63:1-2)

2. Chipembedzo ndikuyesayesa kwa munthu kuti amudziwe Mulungu. Ndi miyambo ndi malamulo, zintchito ndi mau opanda mphamvu. Chipembedzo chimabweretsa imfa ya uzimu.

Mphamvu ya Mulungu ndikuwonetsera poyera kwa chikhumbo Chake chofuna kuziulula Yekha kwa munthu.

Mphamvu ya uzimu ndi Ufumu wa Mulungu umene ukugwira ntchito. Umabweretsa moyo wa uzimu.

3. Zandale, zakusuku, zakunthupi, zachuma, zankhondo, mphamvu ya chipembedzo ndi mphamvu ya za mphamvu.

4. Mateyu 20:25-25

5. Tanthauzo la Baibulo la mau oti “mphamvu” ndi mphamvu za uzimu, kuthekera, kukakamiza ndi kulimbika. Ndi ufumu wa mphamvu kwambiri umene umabweretsa machitachita amphamvu ndi zozizwa. Tanthauzo la Baibulo la mau oti “ulamuliro” ndi ofanana ndi tanthauzo la mau oti “mphamvu.” Amatanthauza kuti mphamvu zololedwa ndi zoyenera kugwira ntchito mmalo mwa wina. Kutenga ulamuliro ndi mchitidwe wowonetsera mphamvu.

6. Gwero la mphamvu za uzimu za m' Baibulo ndi Mulungu Atate, Mulungu Mwana, ndi Mulungu Mzimu Woyera.

7. Lonjezano ndikutengsa lonjezanolo.

8. Mukuyenera kusakha kutenga lonjezano; mukuyenera kumvetsa ndondomeko; mukuyenera kugwiritsa ntchito ndondomeko.

9. Kulapa.

CHAPUTALA 2:

1. Mulungu ananena kamodzi, ndinachimva kawiri: kuti mphamvu ndi yake ya Mulungu. (Masalimo 62:11).
2. Kuchokera chinachake ndi chiyambi chake.
3. Mulungu wowona ndi wamoyo anawonetsedwera mu Baibulo loyera.
4. Mulungu anawonetsera mphamvu Zake pa dziko lapansi munjira zotsatirazi:

Chilengedwe	Yesu Kristu
Chiweruzo	Mzimu Woyera
Chiwombolo	Zizindikiro zamphamvu
Mau Ake olembedwa	Okhulupirira
5. Zonama. Mulungu nde kochokera mphamvu ndi mphamvu zopambana, koma anakhazikitsanso mphamvu zina.
6. Aefeso 1:9-10 ndi 3:11

CHAPUTALA 3:

1. Ndipo kulibe kudabwa; pakuti satana yemwe adzaonetsa ngati mngelo wa kuunika. Chifukwa chake sikuli kanthu kwakukulu ngatinso atumiki ake adzionetsetsa monga atumiki a chilungamo; amene chimariziro chao chidzakhala monga ntchito zao. (2 Akorinto 11:14-15)
2. Pamene Paulo akuyakhula za “kuipa mmiyamba,” amatanthauza kuipa kwa mizimu imene yabaidwa mu machitachita achipembedzo chadzikoli. Amakopera mphamvu yeni yeni ya Mulungu.
3. Fananitsani mmene mwalemba mwachidule ndizomwe zakambidwa mu chaputala 3.
4. Fananitsani mmene mwalemba mwachidule ndi ndondomeko zomwe zaperekedwa mu chaputala 3.

CHAPUTALA 4:

1. Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine kumwamba ndi dziko lapansi. (Mateyu 28:18).
2. Yesu analibe malire. Anali ndi mphamvu kumwamba ndi dziko lapansi. (Mateyu 28:18)
3. Mulungu Atate.
4. Fananitsani mmene mwalembera mwachidule ndi zomwe zakambidwa mu chaputala 4.

CHAPUTALA 5:

1. Taonani, ndakupatsani ulamuliro wakuponda pa njoka nsi zinkhanira, ndi pa mphamvu iri yonse ya mdaniyo; ndipo kulibe kanthu kadzakuipsani konse. (Luka 10:19).
2. Ulamuliro wauzimu waokhulupirira unaperekedwa ndi Yesu.
3. Pamene wina wapatsidwa udindo kuti achite china chake, akuyenera kupatsudwanso ulamuliro ochitira chinthucho.
4. Kukafikira dziko lonse ndi Uthenga Wabwino.
5. Mau a Chigriki oti “dunamis” amatanthauza kuti mphamvu zobadwa nazo. Mau oti “exousia” amatanthauza kuti mphamvu zochita kupatsidwa kapena ulamuliro.
6. Kunenaku mkonama.

CHAPUTALA 6:

1. Ndipo iwowo anaturuka, nalalikira ponse ponse, ndipo Ambuye anachita nao pamodzi natsimikiza mau ndi zizindikiro zakutsatapo. (Marko 16:20).
2. Mphamvu padziko zimagwiritsidwa ntchito ndi zolinga zozikonda. Mphamvu ya uzimu ikuyenera kugwiritsidwa ntchito pa zolinga za uzimu ndi kupititsa ufumu wa Mulungu pamtsogolo.
3. Mateyu 20:25-27
4. Munakalemba chaolinga chilichonse chimene chakambidwa mu chaputala chino.

CHAPUTALA 7:

1. Pakuti Uthenga Wabwino sundichititsa manyazi; pakuti uli mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wakukhulupirira; kuyambira Myuda, ndiposo Mhelene.(Aroma 1:16).
2. Mau oti “Uthenga Wabwino” amatanthauza kuti “uthenga wabwino.” Pamene tikuyakhula za Uthenga Wabwino malinga ndi Baibulo limakhala likutanthauza kuti uthenga wabwino wa Ufumu wa Mulungu ndi chipulumutso kupyolera mwa Yesu Kristu.
3. 1 Akorinto 15:3-4. Maziko eni eni a Uthenga Wabwino amayangana pa moyo ndi utumiki wa Yesu. Izi mkuphatikizapo imfa Yake chifukwa chamachimo a anthu onse, kuikidwa kwake mmanda, ndiposo chiukitso Chake kwa akumfa molinga ndi umboni olembedwa wa Mau a Mulungu.
4. Onani Aroma 1:16-19
 - Ndi bvumbulutso la Mulungu kwa munthu.
 - Umabweretsa chipulumutso kwa anthu onse, posatengera mtundu, nkhungu, kapenaso chikhulupiriro.
 - Umaulula chimene chimayenera kudziwika kwa munthu chokhudzana Mulungu.
 - Umaulula chilango ndi mkwiyo wa Mulungu podana ndi tchimo.
 - Umawonetsa chilungamo cha Mulungu.
 - Umawonetsa mmene ungalungamitsidwire ndi chikhulupiriro.
 - Ndi maziko achikhulupiriro chomwe tikhalira.
5. Fananitsani mmene mwalemba mwachidule pa mphamvu imene iri mwazi kuzokambirana mu Chaputala 7.
6. Chikhulupiriro.
7. Mvomereza kuti munachimwa: Aroma 3:23
 Khulupirirani kuti Yesu anafera machimo anu: Yohane 3:16-17

Mvomerezani machimo anu kwa Mulungu ndipo mupepheni kuti akukhululukireni: 1 Yohane 1:8-9.

Khalani moyoo wosithika : 2 Akorinto 5:17

8. Zabodza. Yesu anapereka moyo wake mofuna pa mtanda.

CHAPUTALA 8:

1. Ndipo onani, Ine nditumiza pa inu lonjezano la Atate wanga; koma khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yochokera kumwamba.(Luka 24:49).
2. Machitidwe 1:8. Mphamvu imabwere pomwe Mzimu Woyera wabwera pa ife.
3. Kutu mukhale mboni ya Ambuye Yesu Kristu. Onani Machitidwe 1:8
4. Agalatiya 5:22-23
5. Rapani ndipo batizidwani
Khulupirirani kuti ndiyanu
Ikhumbireni
Zindikirani kuti ndi mpatso
Ziperekeni kwa Mulungu
Pephani mapephero a okhulupirira ena
6. Fananitsani ndandanda wanu kuzomwe zakambidwa mu Chaputala 8.

CHAPUTALA 9:

1. Ndipo tsopano zitsala chikhulupiriro, chiyembekezo, chikondi, zitanu izi; koma chachikulu cha izi ndicho chikondi.(2 Akorinto 13:13)
2. Chikondi ndi maimvaimva akuya, chisamaliro, ndi kukhudzidwa zomwe zimabwera miyoyo yanthu monga ngati chipatso cha Mzimu Woyera.
3. Lamulo lalikulu loyamba ndi kukonda Mulungu. Lachiwiri ndi kukonda ena. Marko 12:30-31.

4. Chikondi chanthu pa anthu ena. Yohane 13:35
5. Chikondi.
6. Chikondi.
7. Chimodzimodzi ngati chikondi.

CHAPUTALA 10:

1. Ndipo inu, kudzodza munalandira kuchokera kwa Iye, kukhala mwa inu, ndipo simusowa kuti wina akuphunzitseni; koma monga kudzodza kwake kukuphunzitsani za zinthu zonse, ndipo kuli koono, sikuli bodza ayi, ndipo monga kudaphunzitsa inu, mukhale mwa Iye. (1 Yohane 2:27)
2. Kudzodzedwa kopatulika mu Chipangano Chakale kumkagwiritsidwa ntchito popatula anthu ndi zinthu kudzipereka ku ntchito ya Mulungu.
3. Kudzodza kopatulika kumkagwiritsidwa ntchito podzodza aneneri, mafumu, amsembe, magome, kachisi ndi zokhalamo zake.
4. Odzodzedwayo.
5. Fananitsani mmene mwalembera mwachidule zomwe zakambidwa mu Chaputala 10.
6. Chifukwa Mulungu sadzodza aliyense pa utumiki ofanana. Kulephera ndi chisokonezo zimakhala zotsatira pamene mukuyesera kukopera utumiki umene Mulungu sanakudzodzeni nawo inu.
7. Fananitsani mayankho anu ndi ndondomeko zimene zaperekedwa mu Chaputala 10.
8. Mulungu.

CHAPUTALA 11:

1. Ndipo Stefano, wodzala ndi chisomo ndi mphamvu anachita zozizwa ndi zizindikilo zazikulu mwa anthu. (Machitidwe 6:9)
2. Chikhulupiro chimatanthauza kuti kukhulupirira ndi kukhala ndichitsimikizo cha chinthu chinachake. Kukhulupirira kumatanthauza kukhulupirika. Mau oti chikhulupiriro, kukhulupirira, ndikukhulupirira mmalemba amatanthauza chinthu chimodzi.

b. Machiritso

e. Ziwanda

c. Kuyeretsa

f. Kubatiza

8. a. Zowona

b. Zowona

c. Zonama

CHAPUTARA 13:

1. Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukuru m'mschitidwe ake. (Yakobo 5:16b)
2. Pemphero ndikusala kudyā.
3. Kupempha, kufuna, kugogoda.
4. Kulambira ndi kupembedza, kuzipereka, zopepherera, kumvomereza, kupembedzera.
5. Wonani ndandanda mu Chaputala 13.
6. Pemphero ndi kuyanjana ndi Mulungu. Limachitika mosiyana-siyana, koma kwakukuru ndi pamene munthu alankhula ndi Mulungu ndi Mulungu alankhula ndi munthu.
7. Kusala kudyā, mukufotokoza kuphweka, ndi kukhala opanda chakudyā.
8. Molingana ndi Mau a Mulungu, pali mitundu iwiri ya kusala kudyā. Kusala kwa tunthu ndi kusala moyepula. Kusala kwatunthu ndi pomwe munthu sakudyā kapena kumwa chiri chonse Machitidwe 9:9. Kusala moyepula ndi pomwe munthu amangodyako tina ndi tina basi Daniel 10:3.
9. Kukuchepetsani.

Kulapa ku tchimo

Bvumbulutso

Kudula chigwe cha kuipa, kunyamula goli lolemetsa, kumasula opondrezedwa, ndi kuphwasula goli lirironse

Kukwanitsa kudyetsa osauka, kunthupi ndi ku uzimu

Kumva za Mulungu

CHAPUTALA 14:

1. Pakuti Mau a Mulungu ali amoyo ndi ochitachita, ndi akuthwa koposa lupanga lakuthwa konse konse, napyoza kufikira kugawira moyo ndi mzimu, ndi mfundo ndi mafuta a m'mafupa nazindikiritsa zolingalira ndi zitsimikizo za mtima. (Ahebri 4:12)
2. Mulungu.
3. “rhema” Mau a Mulungu amatanthauza zoyakhula zapaderadera za Mulungu zomwe zimagwiritsidwa ntchito pa zochitika zapaderaderaso.
4. “logos” Mau a Mulungu amatanthauza kuyakhula kwa Mulungu kwamphumphu. Ndi bvumbulutso lathuthu la zomwe Mulungu anayakhula.
5. Anakumana nawo ndi Mau a mphamvu. Anagwiritsa ntchito “rhema” Mau a Mulungu.
6. Fananitsani zimene mwalembe mwachidule ndi zomwe zakambidwa mu Chaputala 14.
7. Zabodza.

CHAPUTALA 15:

1. Anthu onse amvere maulamuliro a akulu; pakuti palibe ulamuliro wina komawochokera kwa Mulungu; ndipo iwo amene alipo aikidwa ndi Mulungu. (Aroma 13:1).
2. Mukuyenera kutenga ulamuliro wanu kuchokera kochokera koyenera.
3. Yesu anali panso pa ulamuliro wa Mulungu. Uku kunali kochokera kwa ulamuliro umene amagwiritsa ntchito. Chifukwa cha ichi, Anali ndi ulamuliro pamatenda, ziwanda, tchimo, ndi zonse zachilengedwe.
4. Fananitsani mmene mwalembera mwachidule ndi zomwe zakambidwa mu Chaputala 15.
5. Aroma 13:1-7
6. Mulungu.

CHAPUTALA 16:

1. Kuti ndimzindikire Iye ndi mphamvu ya kuuka kwake, ndi chiyanjano cha zowawa zake, pofaniziridwa ndi imfa yake. (Aefeso 3:10).
2. Tanthauzo la mau oti “chiukitso” ndi kudzuka kapena kudzutsidwa, kudzutsidwa kwa akufa kukhalanso ndi moyo.

3. Fananitsani mmene mwalembere mwachidule ndi zomwe zakambidwa mu Chaputala 16.
4. Zanama.
5. Fananitsani mmene mwalembere mwachidule mwanu ndi zomwe zakambidwa mu Chaputala 16.
6. Yesu. Yohane 11:25

CHAPUTALA 17:

1. Pakuti anapachikidwa m'ufoko, koma ali ndi moyo mu mphamvu ya Mulungu. Pakuti ifenso tiriofoka mwa Iye, koma tidzakhala ndi moyo pamodzi ndi Iye, mu mphamvu ya Mulungu ya kwa inu. (2 Akorinto 13:4)
2. Satana
3. Kuzuzika kumabwera miyoyo yanthu kudzera mwa ena, zochitika za moyo, utumiki, tchimo, ndi machitachita asatana achiwembu.
4. Fananitsani mmene mwalembere mwachidule za zolinga zakuzuzika ndi zomwe zakambidwa mu Chaputala 16.

CHAPUTALA 18:

1. Ndipo iwowo anatuluka, nallikiraponseponse, ndipo Ambuye anachita nao pamodzi, natsimikiza mau ndi zizindikilo zakutsatapo. (Marko 16:20)
2. Fananitsani mmene mwalembere mwachidule ndi zomwe zakambidwa mu Chaputala 18.
3. Mpingo ukuyenera kukhala paphata powonetsera mphamvu ya Mulungu.
4. Mukuyenera kuigwiritsa ntchito kuti ichuluke. Onani faniziro mu Luka 19:12-26.

CHAPUTALA 19:

1. Ndipo Iye, chifukwa chakusakhulupirira kwao, sanachita kumeneko zamphamvu zambiri. (Mateyu 13:58)
2. Deuteronomo 29:29.
3. Fananitsani mmene mwalembere mwachidule ndi zomwe zakambidwa mu Chaputala 19

CHAPUTALA 20:

1. Adzikhazikitsa mafumu adziko lapansi, nachita upo akulu pamodzi, kutsutsana naye Yehova, ndi Wodzodzedwa wake... (Masalimo 2:2)
2. Satana.
3. Fananitsani z=mmene mwalemba mwachidule ndi zomwe zakambidwa mu Chaputala 20.
4. Onani ndondomeko zimene zaperekedwa mu Chaputala 20.